

UTUMIKI
WA
MZIMU WOYERA

HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a **Harvest International Institute** ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

@Harvestime International Institute

ZAMKATI MWA BUKULI

Kagwiritsidwe Nthcito Ka Bukuli.....	3
Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira Limodzi Pagulu.....	4
Mau Oyamba.....	5
Zolinga za Maphunzirowa.....	6
1. Zofotokozera Zoyamba Za Mzimu Woyera.....	7
2. Zinthu Zoimira Mzimu Woyera.....	22
3. Utumiki wa Mzimu Woyera.....	30
4. Ubatizo wa Mzimu Woyera	44
5. Mpatso za Mzimu Woyera.....	58
6. Mphatso zapadera za Mzimu Woyera.....	74
7. Mphatso zolankhula za Mzimu Woyera.....	97
8. Mphatso zotumikira za Mzimu Woyera.....	105
9. Zizindikiro za Mzimu Woyera.....	120
10. Kuzindikira mphatso yanu Yauzimu	134
11. Chipatso cha Mzimu Woyera.....	163
12. Ntchito za thupi.....	182
13. Kukuza chipatso chanu chauzimu.....	200
Zinthu zina zapadera: Ndime zokhudza mphatso zauzimu kuchokera mu Baibulo.....	213
Mayankho amafunso odziyesa nokha.....	214

KAGWIRITSIDWE NTHCITO KA BUKULI

KAKONZEDWE KA BUKULI

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

Zolinga: Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Welangani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

Vesi Yotsogololera: Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

Zopezeka mu Magawo: Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

Mayeso Odziyesa Nokha: Osathamangira kulemamba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

Zophunzira Zowonjezera: Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mau Mulungundi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

Mayeso Omaliza: ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

ZOWELENGA ZINA ZOFUNIKA POHUNZIRA PHUNZIROLI

Mudzafunikira Buku Lopatulika

NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

MKUMANO WOYAMBA

Kutsekulira: Yamabani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu: Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene mudzikumana.

Mayamiko ndi Matamando: Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

Gawani Mabuku Kwa Ophunzira: Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

Perekani Nchito Yoyamba. Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene adziphunzitsidwa pa mkumano uli onse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

Kutsekulira: Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina awophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a wophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

Kukumbutsira: Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

Phunziro: Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphunzira komanso mmene angagwiritsire ntchito zimene aphunzira pamoyo wawo ndi utumiki.

Mayeso Odziyesa Nokha: Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankha kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adziperezere okha mayankho.

Mayeso omaliza: Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphunzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina ali yense ali ndi buku laphunziroli.

Phunziro: Utumiki wa Mzimu Woyera

MAWU OYAMBA

Pa ulendo wina wa utumiki, mtumwi Paulo anafunsa gulu lina lokhulupirira za Mzimu Woyera. Iye anawafunsa ngati analandira Mzimu Woyera kuchokera pomwe iwo anakhulupirira. Koma iwo anayankha kuti “ngakhale zakuti kuli Mzimu Woyera ife sitinamvepo ayi. (Machitidwe 19:2). Paulo anasgawana nawo okhulupirirawa za utumiki wa Mzimu Woyera. (Machitidwe 19). Ngakhale lero lino ndizofunikira kwambiri kuti akhulupiririra amvetsetse za utumiki wa Mzimu Woyera. Mulungua nalonjeza kuti:

Ndipo kudzali m' masiku otsiriza, anena Mulungu, Ndidzathira ca Mzimu wansa pa thupi liri lonse, Ndipo ana anu amuna, ndi akazi adzanenera, Ndipo anyamata anu adzaona masomphenya, Ndi akulu anu adzalota maloto; (Machitidwe 2:17)

Mfundo yakuti Mulungu ali wokonzeka kutsanulira mzimu wake pa ife zikupangitsa kuti phunziroli likhale lofunika. Tikuyenera kumvetsetsa utumiki wa Mzimu Woyera kuti tikhale mbali imodzi ya vumbulutso lapaderaderari la mphamvu ya Mulungu. Chiphunzitso cha Mzimu Woyera ndi chimodzi mwa ziphunzitso zikuluzikulu za Baibulo. Paulo anati:

Kufikira ndidza ine, usamalire kuwerenga, kucenjeza, kulangiza. (1 Timoteo 4:13)

Mulungu samagwiritsa ntchito mphamvu za umunthu zachilengedwe poyenda m' dziko lathuli. Izi zimatheka ndi utumiki wa Mzimu Woyera.

Pamenepo anayankha, nanena kwa ine, ndi kuti, Awa ndi mau a Yehova kwa Zerubabele, Ndi khamu la nkondo ai, ndi mphamvu ai, koma ndi Mzimu wanga, ati Yehova wa makamu. (Zekariya 4:6)

Phunziroli lifotokoza za chilengedwe cha Mzimu Woyera komanso umunthu wake. Phunziroli likufotokoza za maina omwe Mzimu Woyera amadziwika nawo. Mainawa amawulula za utumiki wa Mzimu Woyera. Zolinga, mphatso ndi chipatso cha Mzimu Woyera zaunikiridwanso mwatsatanetsatane. Njira zothandiza zaperekedwa kuti mubatizidwe ndi Mzimu Woyera, kuzindikira mphatso za Mzimu Woyera ndikuwonetsa chipatso cha Mzimu Woyera.

ZOLINGA ZA PHUNZIROLI

Pamapeto paphunziro ili mukwanitse kuchita izi:

- Kufotokozera umunthu wa Mzimu Woyera
- Kupeza maina osiyanasiyana oyimira Mzimu Woyera
- Kupeza zizindikiro zoyimira Mzimu Woyera
- Kufotokozera utumiki wa Mzimu Woyera
- Kufotokozera momwe munthu angalandirire ubatizo wa Mzimu Woyera
- Mulandire Mzimu Woyera
- Perekani mphatso za Mzimu Woyera ndi matanthauzo ake
- Pezani mphatso zanu za Mzimu Woyera
- Pezani chipatso cha Mzimu Woyera
- Pezani ntchito za thupi
- Onetsani chipatso cha Mzimu Woyera m'moyo wanu

CHAPUTALA 1

ZOFOTOKOZERA ZOYAMBA ZA MZIMU WOYERA

ZOLINGA:

Pomaliza pa phunziro ili mukwanitse kuchita izi:

- Kupeza Mzimu Woyera ngati gawo limodzi la utatu wa Mulungu
- Kupereka zomwe zikuyimira umunthu wa Mzimu Woyera
- Kufotokoza chilengedwe cha Mzimu Woyera

Mavesi otsogolera:

Ndipo Yesu, pamene anabatizidwa, pomwepo anaturuka m'madzi: ndipo onani, miyamba inamtsegukira Iye, ndipo anapenya Mzimu wa Mulunguwakutsika ngati nkhunda nudza nutera pa Iye; ndipo onani, mau akucokera kumiyamba akuti, Uyu ndiye Mwana wanga wokonedwa, mwa Iyeyu ndikondwera. (Mateyu 3:16-17

MAU OYAMBA

Chaputala ichi chikufotokozera chiyambi cha Mzimu Woyera. Chikufotokozera malo ake mu utatu wa mulungu, zimene zimayimira umunthu wake wa Mzimu Woyera, komanso kuchenjeza za kunzindikira kwake. Mlowammalo “iye” akugwiritsidwanso ntchito kusonyeza kuti Mzimu Woyera ndi m’modzi mwa utatu wa mulungu.

Yesu anayankhula za Mzimu Woyera ngati “iye”. Yesu anati;

-Iye adzayankhula za ine. Yohane 15:26

-Ndidzamtumiza iye kwa inu. Yohane 16:7

-Iye adzalemekeza ine. Yohane 16:14

-Iye sadzayankhula za iye mwini. Yohane 16:13

UTATU WA MULUNGU

Pali milungu Yambirimbiri yomwe imapembedzedwa mu dziko lonse lapansi. Koma pali Mulungu m’modzi yekha wowona. Mu m’baibulo muli nkhanu ya Mulungu wowona ameneyu. Baibulo ndi mawu a Mulungu ndipo limawulula ndondomeko yapaderadera ya Mulungu pa anthu onse.

Chimodzi mwa zinthu zimene Baibulo limawulula ndi utatu wa Mulungu. Izi zikutanthauza kuti umunthu wake umawonekera mu magawo atatu. Iye ndi Mulungu mmodzi mwa atatu. Mzimu Woyera ndi mmodzi mwa utatu wa Mulungu omwe ndi Mulungu atate, Mulungu mwana ndi Mulungu Mzimu Woyera.

Gawo lirilonse la utatu wa Mulungu; Mulungu atate, Mulungu mwana ndi Mulungu Mzimu Woyera lili ndi ntchito yake yapaderadera pa anthu. Phunziro ili likhazikika pa utumiki wa Mzimu Woyera ndi cholinga chake.

MULUNGU MZIMU WOYERA

Mzimu Woyera akutchedwa kuti “Mulungu”.

Koma Petro anati, Hananiya, Satana anadzaza mtima wako cifukwa ninji kudzanyenga Mzimu Woyera, ndi kupatula pa mtengo wace wa mundawo? Pamene unali nao, sunali wako kodi? ndipo pamene unaugulitsa sunali m'manja mwako kodi? bwanji cinalowa ici mumtima mwako? sunanyenga anthu, komatu Mulungu. (Macitidwe 5:3-4)

Chifukwa chakuti Mzimu Woyera akutchedwa kuti “Mulungu”, iye ndiwofanana ndi Mulungu atate komanso Mulungu mwana. Mavesi otsogolera a chaputala chino akuwulula momveka bwino za utatu wa mulungu. Yesu akubatzidwa, Mzimu Woyera akutsika ndipo Mulungu akuyankhula;

Ndipo Yesu, pamene anabatizidwa, pomwepo anaturuka m'madzi: ndipo onani, miyamba inamtsegukira Iye, ndipo anapenya Mzimu wa Mulungu wakutsika ngati nkhunda nudza nutera pa Iye; ndipo onani, mau akucokera kumiyamba akuti, Uyu ndiye Mwana wanga wokonedwa, mwa Iyeyu ndikondwera. (Mateyu 3:16-17)

Atatsala pang'ono kubwerera kumwamba atamaliza utumiki wake pa dziko lapansi pano, Yesu anayankhula za Mzimu Woyera ;¹

Koma pamene wafika Nkhoswe, amene Ine ndidzamtuma kwa inu kucokera kwa Atate, ndiye Mzimu wa coonadi, amene aturuka kwa Atate, Iyeyu adzandicitira Ine umboni. (Yohane 15:26)

Mtumwi Paulo anayankhula za utatu wa mulungu:

Pakuti cilamulo ca mzimu wa moyo mwa Kristu Yesu candimasula ine ku lamulo la ucimo ndi la imfa. Pakuti cimene cilamulo sicinathe kucita, popeza cinafoka mwa thupi, Mulungu anatumiza Mwana wace wa iye yekha m'cifanizo ca thupi la ucimo, ndi cifukwa ca ucimo, natsutsa ucimo m'thupi; Aroma 8:2-3

Cisomo ca Ambuye Yesu Kristu, ndi cikondi ca Mulungu, ndi ciyanjano ca Mzimu Woyera zikhale ndi inu nonse. (2 Akorinto 13:14)

kuti mwa iye ife tonse awiri tiri nao malowedwe athu kwa Atate, mwa Mzimu mmodzi. (Aefeso 2:18)

¹ *Phunziro la Mulungu atate ndi Mulungu mwana laperekedwa mu buku lapadera la *Harvestime International Institute* mu phunziro la *Ndondomeko ya Nkhondo Yauzimu*. Ndondomeko za chiphunzitso cha Mulungu atate ndi Mulungu mwana zaperekedwa pa mbali ya “maphunziro owonjezera” kumapeto kwa chaputalachi.

**Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: a dziko...
(Macitidwe 1:8)**

WAMUYAYA (ETERNAL)

Iye ndi wamuyaya, alibe chiyambi ndipo sadzakhala ndi chimaliziro.

**koposa kotani nanga mwazi wa Kristu amene anadzipereka yekha wopanda cirema
kwa Mulungumwa Mzimu wosatha, udzayeretsa cikumbu mtima canu kucisiyanitsa
ndi nchito zakufa, kukatumikira Mulunguwamoyo? (Ahebri 9:14)**

Umuyaya wa Mzimu Woyera utha kuwonetsedwa ndi seko. Seko simawonetsa poyambira kapena pothera, kamabe imawoneka kuti ilipo.



Umuyaya wa Mzimu Woyera

UMUNTHU WA MZIMU WOYERA

Mzimu Woyera ndi gawo limodzi la utatu wa Mulungu, komabe Mzimu Woyera ali ndi umunthu wake. Baibulo limanena kuti Mzimu Woyera ali ndi ...

AMAGANIZA:

Ndipo iye amene asanthula m'mitima adziwa cimene acisamalira Mzimu, cifukwa apempherera oyera mtima monga mwa cifuno ca Mulungu. (Aroma 8:27)

AMAFUFUZA MALINGALIRO A MUNTHU

Koma kwa ife Mulungu anati onetsera izi mwa Mzimu; pakuti Mzimu asanthula zonse, zakuya za Mulungu zomwe. (1 Akorinto 2:10)

ALI NDICHIFUNIRO:

Koma kwa ife Mulunguanati onetsera izi mwa Mzimu; pakuti Mzimu asanthula zonse, zakuya za Mulunguzomwe. (1 Akorinto 2:10)

Chifuniro cha Mzimu Woyera chimatsogolera okhulupirira powakaniza kuchita zinthu zina:

Ndipo anapita pa dziko la Frugiya ndi Galatiya, atawaletsa Mzimu Woyera kuti asalalikire mau m'Asiya; pamene anafika kundunji kwa Musiya, anayesa kunka ku Bituniya; ndipo Mzimu wa Yesu sanawaloleza; (Macitidwe 16:6-7)

Mzimu Woyera amatsogoleranso okhulupirira powapatsa chilolezo:

Pamene anaona masomphenyawo, pomwepo tinayesa kuturukirakunka ku Makedoniya, poganizira kuti Mulunguanaitanira ife kulalikira Uthenga Wabwino kwa iwo. (Macitidwe 16:10)

AMAYANKHULA

Anayankhula kwa Filipo:

**Ndipo Mzimu anati kwa Filipo, Yandikira, nudziphatike ku gareta uyu.
(Macitidwe 8:29)**

Anayankhula kwa Petulo:

Ndipo m'mene Petro analingirira za masomphenya, Mzimu ananena naye, Taona, amuna atatu akufuna iwe. (Macitidwe 10:19)

Anayankhula kwa akulu ampingo aku Antiyokeya:

**Ndipo pa kutumikira Ambuye iwowa, ndi kusala cakudya, Mzimu Woyera anati, Mundipatulire Ine Bamaba ndi Saulo ku nchito imene odinawaitanirako.
(Macitidwe 13:2)**

Chivumbulutso chaputala 2 ndi 3 chikuwonetsera zomwe Mzimu Woyera anayankhula ku mipingo isanu ndi iwiri ya ku Asiya.

AMAKONDA

Ndipo ndikudandaulirani, abale, ndi Ambuye wathu Yesu Kristu, ndi cikondi ca Mzimu, kuti 5 mudzalimbike pamodzi ndi ine m'mapemphero anu kwa Mulungucifukwa ca ine; (Aroma 15:30)

AMATIPEMPHERERA:

Umunthu wina wa Mzimu Woyera ndi wakuti iye ndi wopembedzera. Izi zikutanthuza kuti iye amapemphera kwa Mulungu mmalo mwa ena:

Ndipo momwemonso Mzimu athandiza kufoka kwathu; pakuti cimene tizipempha monga ciyenera, sitidziwa; koma Mzimu mwiniatipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka; (Aroma 8:26)

KUZINDIKIRA KWA MZIMU WOYERA

Mzimu Woyera ali ndi chilengedwe chozindikira. Izi zikutanthauza kuti iye ali ndi maimvaimva ndipo amakhudzidwa ndi zochita za munthu. Chifukwa cha chilenge chake chozindikira, Baibulo timatichenjeza kuti tisachite izi:

KUNAMIZA MZIMU WOYERA:

**Koma Petro anati, Hananiya, Satana anadzaza mtima wako cifukwa ninji kudzanyenga Mzimu Woyera, ndi kupatula pa mtengo wace wa mundawo? Pamene unali nao, sunali wako kodi? ndipo pamene unaugulitsa sunali m'manja mwako kodi? bwanji cinalowa ici mumtima mwako? sunanyenga anthu, komatu Mulungu.
(Machitidwe 5:3-4)**

KUSAMVERA ZOFUNA ZA MZIMU WOYERA:

Ouma khosi ndi osadulidwa mtima ndi makutu inu, mukaniza Mzimu Woyera nthawi zonse; monga anacita makolo anu, momwemo inu. (Macitidwe 7:51 22)

KUZIMA MZIMU:

Mumazima Mzimu Woyera pamene mukukana kuchita zomwe woyera akufuna kuti inu muchite. Mawu oti “kuzima” anagwiritsidwaponso penapake m’baibulo omwe amatanthauza kuti kuzimitsa moto. Mukazima Mzimu Woyera iye amasiya kuyenda kwa mphanvu yake mwa inu. Zili ngati kuthira madzi pamoto. Baibulo limachenjeza kuti:

Musazime Mzimuyo; (1 Atesalonika 5:19)

KUKWIYITSA MZIMU WOYERA

Kuzima Mzimu Woyera ndi kusachita zimene iye akufuna kuti ife tichite. Kukwiyitsa Mzimu Woyera ndikuchita zimene woyera sakufuna kuti ife tichite. Ana a Israeli anakwiyitsa Mzimu Woyera:

Kawiri kawiri nanga anapikisana ndi Iye kucigwako, Nammvetsa cisoni m'cipululu. (Masalmo 78:40)

Baibulo limachenjeza kuti:

Ndipo musamvetse cisoni Mzimu Woyera wa Mulungu, amene munasindikizidwa cizindikilo mwa iye, kufikira tsiku la maomboledwe. (Aefeso 4:30)

KUNYOZA MZIMU WOYERA

Mumanyoza Mzimu Woyera pakubwereranso ku uchimo mutatha kukhululukidwa machimo kudzera mwa mwazi wa Yesu Mkhristu:

ndipo mutani, kulanga koposa kotani nanga adzayesedwa woyenera iye amene anapondereza Mwana wa Mulungu, nayesa mwazi wa cipangano umene anayeretsedwa nao cinthu wamba, z nacitira cipongwe Mzimu wa cisomo; (Ahebri 10:29)

Pakuti sikutheka kuwakonzanso, atembenuke mtima, iwo amene anaunikidwa pa nthawi yace, nalawa mphatso ya Kumwamba, nakhala olandirana naye Mzimu Woyera, nalawa mau okoma a Mulungu, ndi mphamvu ya nthawi irinkudza, koma anagwa m'cisokero; popeza adzipaeikiranso okha Mwana wa Mulungu, namcititsa manyazi poyera. (Ahebri 6:4-6)

KUYANKHULIRA MWANO MZIMU WOYERA:

Cifukwa cace ndinena kwa inu, Macimo onse, ndi zonena zonse zamwano, zidzakhululukidwa kwa anthu; koma camwano ca pa Mzimu Woyera sicidzakhululukidwa. Ndipo amene ali yense anganenere Mwana wa munthu zoipa, adzakhululukidwa; koma amene ali yense anganenere Mzimu Woyera zoipa sadzakhululukidwa nthawi yino kapena irinkudzayo. (Mateyu 12:31-32)

Uchimo woyankhulira mwano Mzimu Woyera umatchedwa kuti “tchimo losakhululukidwa”. Molingana ndi ndime imeneyi ndi tchimo lokhalo lomwe ndilosakhululukidwa. Kuyankhulira mwano Mzimu Woyera ndikuyankhula mawu achipongwe okana mphanvu ya Mzimu Woyera ngati mphanvu ya Mulungu ndikumanena kuti ndi mphanvu ya satana. Ngati munthu akanitsitsa mphanvu ya Mzimu Woyera ndiye kuti munthu ameneyu sangathe kupulumuka chifukwa chakuti ndi Mzimu Woyera amene amafikitsa anthu ochimwa chifupi ndi Yesu mkhristu.

Mzimu Woyera amawonetsa zizindikiro zowoneka kutsimikizira mphanvu ya Mulungu. Yesu anayankhula kuti ngati savomereza zizindikiro zozizwitsazi ngati chitsimikizo cha choonadi cha uthenga wabwino, ndi chaninso china chomwe angakhutitsidwe nacho kuti akhulupirire?

KUMVETSA CHISONI MZIMU WOYERA

Kumvetsa chisoni Mzimu Woyera zikutanthauza kuti kukhumudwitsa, kumuwukira kapena kukwiyitsa. Mzimu Woyera amamva chisoni ndi kusamvera komanso kusakhulupirira kwa anthu. Mneneri Yesaya akufotokoza zomwe zinachitika pamene ana a Israeli anamvetsa chisoni Mzimu Woyera:

Koma iwo anapandukira ndi kumvetsa cisoni mzimu wace woyera, cifukwa cace Iye anasandulika mdani wao, nawathira nkhondo Iye yekha. (Yesaya 63:10)

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osawonera.

2. Mzimu Woyera ndi gawo limodzi la utatu wa Mulunguyemwe ndi Mulungu _____, Mulungu _____, ndi Mulungu _____.

3. Perekani umunthu wa Mzimu Woyera usanu ndi umodzi womwe wafotokozeredwa mu chaputala chimenechi:

4. Kodi mawu akuti Mzimu Woyera “amazindikira” akutanthauza chani?

5. Chifukwa chakuti Mzimu Woyera “amazindikira”, Baibulo likuchenjeza kuti tisachite izi:

_____ kwa Mzimu Woyera _____ mzimu. _____ mzimu.
_____ mzimu. _____ mzimu. _____ mzimu.
_____ mzimu.

6. Werengani mawu mu mndandanda woyamba ndi matanthauzo ake mu mndandanda wachiwiri. Lembani nambala yatanthauzo kutsogolo kwa mawu amene akufotokozerera moyera. Yoyamba yaperekedwa ngati chitsanzo.

UTATU WA MZIMU WOYERA

Mndandanda Woyamba

Mndandanda Wachiwiri.

___5___ Ofanana 1. Zikutanthauza kuti iye ndi wamphamvu yonse.

___ ___ Opezeka paliponse 2. Zikutanthauza kuti iye amadziwa zones.

___ ___ Odziwa zonse. Zikutanthauza kuti iye amapezeka paliponse.

___ ___ Wamphamvu zonse. Zikutanthauza kuti iye ndi wamuyaya.

___ ___ Wamuyaya 5. Zikutanthauza kuti iye ali mmodzi ndi atate ndi mwana.

(Mayankho amafunso amenewa aperekedwa kumapeto kwa chaputala chomaliza cha bukuli)

ZOWONJEZERA POPHUNZIRA

Mutu wa phunziro lino ndi Mzimu Woyera amene ndi mmodzi mwa utatu wa mulungu. Mndandanda uli mmusiwu ukuthandizani kuphunzira za Mulungu Atate ndi Mulungu mwana.

UTATU WA MULUNGUWOYERA

Mulungu ndi mmodzi mwa atatu, Atate mwana ndi Mzimu Woyera.

- Atate amachitira umboni mwana Mateyu 3:17
- Mwana amachitira umboni Atate Yohane 5:19-20
- Mwana amachitira umboni mzimu Yohane 14:26

MULUNGUATATE

Mulungundi mlengi wa zonse: Nehemiya 9:6

MAINA A MULUNGU:

Mawu oti “mulungu” [amene amapembedzedwa] ndi dzina limene anthu amagwiritsa ntchito pomutchula iye amene ali wapamwamba pa onse. Baibulo limapereka maina ena ambiri a mulungu. Maina a Mulungusiwongotchulira Mulunguayi koma mainawo amatambasula chomwe dzinalo likutanthauza. Ena mwa maina a Mulungundi awa:

Yehova: kutanthauza kuti Ambuye. Baibulo limaphatikiza dzinali ndi maina ena monga awa:

Yehova-Rafa: kutanthauza kuti yehova wochiritsa nthenda eksodo 15:26

Yehoha-nisi: kutanthauza kuti Mulunguwomenya nkondo eksodo 17:8-15

Yehova-Shalomu: "Ambuye mtendere wathu": Oweruza 6:24

Yehova-Ra'ah: "Yehova ndiye m'busa wanga": Masalimo 23:1

Yehova-Tsidkenu: "Yehova ndiye kulungama kwathu": Yeremia 23:6

Yehova-Jaire: "Yehova wopereka": Genesis 22:14

Jehovah-Shamma: "Yehova wachikhalire": Ezekieli 48:35

Elohimu: kutanthauza kuti mulungu; limagwiritsidwa ntchito pamene mphamvu yolenga ya

Mulunguyawonetsedwa:

Atate: Machitidwe 17:28; yohane 1:12-13

Adonai: kutanthauza kuti Ambuye: Eksodo 23:17; yesaya 10:16,33

El: Dzinali kawirikawiri limagwiritsidwa ntchito pamodzi ndi maina ena:

El Shaddai: "Mulunguamene ndi wokwanira pa zofuna za anthu ake": Eksodo 6:3

Eloham: "Mulunguwamuyaya": Genesis 21:33

El Eliyoni: "Mulunguwambambambamba, wokwezedwa pamwamba pa milungu ina yonse":
Genesis 14:18-20

Chipangano chakale chidalembedwa mu chiyankhulo cha chiheberi, ndipo mum'chiyankhulochi mawu oti "Yahweh" amatanthauza kuti "Mulungu". Mawuwa aphantikizidwa ndi mawu ena ambiri amene akusonyeza chikhalidwe cha mulungu. Mulungundi:

-Yahweh-Jaire: "Yehova wopereka": Genesis 22:14

-Yahweh-nisi: kutanthauza kuti Mulunguwomenya nkondo eksodo 17:15

-Yahweh-Shalomu: "Ambuye mtendere wathu": Oweruza 6:24

-Yahweh Sabbaoth: "Yehova wamakamu": I Samueli 1:3

-Yahweh Maccaddeshcem: "Yehova wondiyeretsa": Eksodo 31:13

-Yahweh Roi: "Yehova ndiye m'busa wanga": masalimo 23:1

-Yahweh-Tsidkenu: "Yehova ndiye kulungama kwathu": Yeremia 23:6

-Yahweh Shammah: "Yehova wachikhalire": Ezekieli 48:35

-Yahweh Elohimu Israeli: "Yehova Mulunguwa Israeli": Oweruza 5:3

-Quadosh Israeli: "Oyera wa Israeli": Yesaya 1:4

MULUNGUALI KUTI?

Mpando wachifumu wa Mulunguuli kumalo otchedwa kumwamba. Koma iye amakhalanso mu dziko lonse (lapansi ndi la kumwamba). Mulunguamapezeka paliponse: II Mbiri 16:9; Yesaya66:1; Miyambo 15:3; masalimo 139:7-8

KODI KUKULA KWA MULUNGUNDI KOTANI?

Mulungundi wamkulu kuposa dziko lapansi ndi la kumwamba. Palibe chida chimene chingawiritsidwe ntchito kuyeza kukula kwa mulungu. Yesaya 40:12,15,22

ZOMWE MULONGUAMADZIWIKA NAZO

Zomwe Mulunguamadziwika nazo zaperekedwa m'musimu. Mulungundi:

Mzimu: Yohane 4:24

Wopanda malire: [Iye alibe malire ngati amene anthu amakhala nawo]: I Mafumu 8:27; Eksodo 15:18; Deuteronomo33:27; Nehemia 9:5; masalimo 90:2; Yeremia 10:10; Chivumbulutso 4:8-10

Mmodzi: Izi zikutanthauza kuti iye ndi Mulungum'modzi mwa atatu: Eksodo 20:3; Deuteronomo 4:35,39;6:4; I Samueli 2:2; II Samueli 7:22; I mafumu 8:60; II mafumu 19:15; Nehemia 9:6; yesaya 44:6-8; I Timoteo 1:17

Wamphamvu yonse: Genesis 1:1; 17:1; 18:14; Eksodo 15:7; Deuteronomo 3:24; 32:39; I mbiri 16:25; yobu 40:2; yesaya 40:12-15; yeremia 32:17; Ezekieli 10:5; Danieli 3:17; 4:35; Amosi 4:13; 5:8; Zakaria 12:1; Mateyu 19:26; chivumbulutso 15:3; 19:6.

Wopezeka paliponse: Genesis 28:15-16; Deuteronomo 4:39; yoswa 2:11; miyambo 15:3; yesaya 66:1; yeremia 23:23-24; Amosi 9:2-4,6; Machitidwe 7:48-49; Aefeso 1:23.

Odziwa zonse: Genesis 18:18,19; II Mafumu 8:10,13; I Mbiri 28:9; masalimo 94:9; 139:1-16; 147:4-5; Miyambo 15:3; Yesaya 29:15-16; 40:28; Yeremia 1:4,5; Ezeieli 11:5; Danieli 2:22,28; Amosi 4:13; Luka 16:15; Machitidwe 15:8,18; Aroma 8:27,29; I Akolinto 3:20; II Timoteo 2:19;4:13; I Peturo 1:2; I yohane 3:20.

Wanzeru: masalimo 104:24; miyambo 3:19; yeremia 10:12; Danieli 2:20-21; Aroma 11:33; I Akolinto 1:24,25,30; 2:6-7; Aefeso 3:10; Akolose 2:2-3.

Woyera: Eksodo 15:11; Levitiko 11:44-45; 20:26; Yoswa 24:19; I Samueli 2:2; Masalimo 5:4; 111:9; 145:17; Yesaya 6:3; 43:14-15; Yeremia 23:9; Luka 1:49; Yakobo 1:13; I Peturo 1:15-16; chivumbulutso 4:8; 15:3-4.

wokhulupirika: Eksodo 34:6; Numeri 23:19; Deuteronomo 4:31; Yoswa 21:43-45; 23:14; I Samueli 15:29; Yeremia 4:28; Yesaya 25:1; Ezeieli 12:25; Danieli 9:4; Mika 7:20; Luka 18:7-8; Aroma 3:4; 15:8; I Akolinto 1:9; 10:13; II Akolinto 1:20; I Atesalonika 5:24; II Atesalonika 3:3; II Timoteo 2:13; Aheberi 6:18; 10:23; I Peturo 4:19; Chivumbulutso 15:3.

Wachifundo: Titus 3:5; Maliro 3:22; Danieli 9:9; Yeremia 3:12; Masalimo 32:5; Yesaya 49:13; 54:7.

Wachikondi: Deuteronomo 7:8; Aefeso 2:4; Zakaliya 3:17; Yesaya 49:15-16; Aroma 8:39; Hosea 11:4; Yeremia 31:3

Wabwino: Masalimo 25:8; Nahumu 1:7; Masalimo 145:9; Aroma 2:4; Mateyu 5:45; Masalimo 31:19; Machitidwe 14:17; Masalimo 68:10; 85:5.

MULUNGU MWANA, YESU KHRISTU

MOYO WA YESU KHRISTU:

Nkhani ya Yesu khristu, Mulungumwana, zalembedwa m'mabuku a Mateyu, Maliko, Luka ndi Yohane.

Werengani mabukuwa kuti mukhale ndi chithunzithunzi chokwanira cha kubadwa, moyo, kuwuka ndi ziphunzitso za Yesu mkhristu.

MAYINA OPEREKEDWA KWA YESU KHRISTU:

Dzina lakuti “Yesu” limatanthauza kuti “mpulumutsi”: Mateyu 1:21

Dzina loti “Khristu” limatauzza kuti “wodzodzedwa”: Yohane 3:34

Maina ena opatsidwa kwa Yesu Khristu m'Baibulo:

-M'busa wabwino: yohane 10:11

-Kuwala kwa dziko lapansi: yohane 8:12

-Mkate wa moyo: yohane 6:48

-Njira: yohane 14:6

-Choonadi: yohane 14:6

-Moyo: yohane 14:6

-Mfumu ya mafumu ndi Mbuye wa ambuye: Chivumbulutso 19:16

-Mwana wa munthu: Mateyu 17:22

-Mwana wa Davite: Mateyu 1:1

-Adamu otsiriza: I Akolinto 15:45

-Kuwala kwa dziwa la m'mawa kochokera kumwamba: Luka 1:78

-Mwana wa Mulungu: Mateyu 16:16

-Mwana wokonedwa: Yohane 3:16

-Mwala wa pangodya: Aefeso 2:20

-Wamsembe wamkulu: Aheberi 4:14

-M'khalapakati: Aheberi 12:24

-Mkango wa fuko la Yuda: Chivumbulutso 5:5

-Oyamba ndi wotsiriza: Chivumbulutso 1:8

-Oweruza olungama: II Timoteo 4:8

-Mfumu ya Ayuda: Marko 15:26

- Mfumu ya israeli: Yohane 1:49
- Woyamba ndi otsiriza wa chikhulupiriro chathu: Aheberi 12:2
- Odala ndi olamula: I Timoteo 6:15
- Mfumu ya moyo: Machitidwe 3:15
- Wotsogolera chipulumutso: Aheberi 2:10
- Ambuye: Machitidwe 2:36
- Mpulumutso: Yohane 4:42
- Khristu: Marko 1:1
- Mawu: Yohane 1:1,14
- Mwana wa Nkhosa wa Mulungu: Yohane 1:29.

ZOMWE YESU AMADZIWIKA NAZO:

Chifukwa chakuti iye ndi gawo limodzi la utatu wa Mulungu, zomwe Yesu Khristu amadziwika nazo ndi zofanana ndi zomwe atate amadziwika nazo. Baibulo limawonetsera zomwe Yesu Khristu amadziwika nazo makamaka m'mavesi otsatirawa:

- Wamphamvu yonse: Mateyu 28:18
- Odziwa zonse: Mateyu 16:30; Yohane 21:17
- Opezeka paliponse: Mateyu 18:20; 28:20
- Wamuyaya: Yohane 1:1-2; 8:58
- Wosasintha: Aheberi 13:8

UMulunguwa Yesu khristu:

Buku la yohane limatsindika za uMulunguwa Yesu khristu, chenicheni ndi chakuti iye ndi gawo limodzi la utatu wa mulungu. Chaputala chilichonse chawonetsera za uMulunguwa Yesu mkhristu. Werengani ma vesi omwe asankhidwa m'musimu ndipo mulembe mwachidule m'mipata yomwe yaperekedwayi:

- 1:49 _____ 11:27 _____
- 2:11 _____ 12:32 _____
- 3:16 _____ 13:13 _____

4:26 _____ 14:11 _____

5:25 _____ 15:1 _____

6:33 _____ 16:28 _____

7:29 _____ 17:1 _____

8:58 _____ 18:11 _____

9:37 _____ 19:7 _____

10:30 _____ 20:28 _____

21:14 _____

CHAPUTALA 2

ZINTHU ZOIMIRA MZIMU WOYERA

ZOLINGA ZA PHUNZIROLI:

Pamapeto pa phunziro ili mukwanitse kuchita izi:

- kupeze zomwe zimayimira Mzimu Woyera.
- Fotokozani chizindikiro chilichonse chomwe chimayimira Mzimu Woyera.
- Perekani maina a Mzimu Woyera.

VESI YOTSOGOLERA:

Kodi simudziwa kuti muli Kacisi wa Mulungu, ndi kuti Mzimu wa Mulunguagonera mwa inu? (1 Akorinto 3:16)

MAWU OYAMBA

Maina komanso zizindikiro zimene zimayimira Mzimu Woyera zimapereka chidziwitso za m'mene iye alili komanso ntchito zake pamoyo wa munthu wokhulupirira. Maina komanso zizindikiro zimene zimayimira Mzimu Woyera ndiye mutu wa chaputala chino pamene tikupitiriza chiyambi cha utumiki wa Mzimu Woyera.

MAINA A MZIMU WOYERA

Dzina (udindo) limayimira udindo umene munthu alinawo kapena ntchito imene iye amagwira. Mwachitsanzo ngati munthu ali ndi dzina la “pulezidenti wa dziko”, izi zimasonyeza udindo womwe iye alinawo mu boma ndi ntchito yomwe iye amagwira ngati m'tsogoleri wa dziko.

Maina amene aperekedwa kwa Mzimu Woyera amayimira udindo wake ndi ntchito yomwe iye amagwira. Mzimu Woyera ndi:

MZIMU WA MULUNGU

Kodi simudziwa kuti muli Kacisi wa Mulungu, ndi kuti Mzimu wa Mulunguagonera mwa inu? (1 Akorinto 3:16)

MZIMU WA KHRISTU:

Koma inu simuli m'thupi ai, koma mumzimu, ngatitu Mzimu wa Mulunguakhalabe mwa inu. Koma ngati munthu alibe Mzimu wa Kristu, siali wace wa Kristu. (Aroma 8:9)

MZIMU WA MUYAYA:

Izi zikutanthauza kuti iye ndi wamuyaya, alibe chiyambi komanso mathero.

koposa kotani nanga mwazi wa Kristu amene anadzipereka yekha wopanda cirema kwa Mulungumwa Mzimu wosatha, udzayeretsa cikumbu mtima canu kucisiyanitsa ndi nchito zakufa, kukatumikira Mulunguwamoyo?? (Ahebri 9:14)

MZIMU WA CHOONADI:

Mzimu Woyera ndi gwero la choonadi chimene chinawuzira mawu a Mulungu, Baibulo. Amawulira choonadi kwa anthu:

Koma atadza Iyeyo, Mzimu wa coonadi, adzatsogolera inu m'coonadi conse; pakuti sadzalankhula za iye mwini; koma zinthu ziri zonse adzazimva, adzazilankhula; ndipo zinthu zirinkudza adzakulalikirani. (Yohane 16:13)

MZIMU WACHISOMO:

ndipo mutani, kulanga koposa kotani nanga adzayesedwa woyenera iye amene anapondereza Mwana wa Mulungu, nayesa mwazi wa cipangano umene anayeretsedwa nao cinthu wamba, z nacitira cipongwe Mzimu wa cisomo; (Ahebri 10:29)

MZIMU WA MOYO:

Pakuti cilamulo ca mzimu wa moyo mwa Kristu Yesu candimasula ine ku lamulo la ucimo ndi la imfa. (Aroma 8:2)

MZIMU WA ULEMELERO:

Mukatonzedwa pa dzina la Kristu, odala inu; pakuti Mzimu wa ulemerero, ndi Mzimu wa Mulunguapuma pa inu. (1 Petro 4:14)

MZIMU WA MZERU NDI VUMBULUTSO:

Mzimu Woyera umapereka mzeru kwa okhulupirira ndi kuwulula chidziwitso cha Yesu mkhristu:

kuti Mulunguwa Ambuye wathu Yesu Kristu, Atate wa ulemerero, akupatseni inu mzimu wa nzeru, ndi wa bvumbulutso kuti mukamzindikire iye; (Aefeso 1:17)

MTONTHOZI:

Mzimu Woyera amatonthoza okhulupirira mu nyengo yamavuto, ya chisoni ndi undekha:

Koma 2 Nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m'dzina langa, (Yohane 14:26)

MZIMU WALONJEZO:

Mzimu Woyera ndi mzimu wamalonjezono chifukwa chakuti iye anatumizidwa kudzakwaniritsa lonjezola Mulungu:

Ndipo e posonkhana nao pamodzi, anawalamulira asacoke ku Yerusalemu, komatu alindire lonjezono la Atate, limene, anati, munalimva kwa Ine; pakuti Yohane

anabatizadi ndi madzi; koma inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera, asanapite masiku ambiri. (Macitidwe 1:4-5)

MZIMU WACHIYERO:

amene anatsimikizidwa ndi mphamvu kuti ndiye Mwana wa Mulungumonga mwa Mzimu wa ciyero, ndi kuuka kwa akufa; ndiye Yesu Kristu Ambuye wathu;(Aroma 1:4)

MZIMU WACHOONADI:

ponamizidwa, tipempha; takhala monga zonyansa za dziko lapansi, litsiro la zinthu zonse, kufikira tsopano, (1 Akorinto 4:13)

MZIMU WA MUWOMBOLI:

Kudzera mwa Mzimu Woyera “tawomboledwa” mu banja la Mulungungati ana a mulungu:

Pakuti inu simunalandira mzimu wa ukapolo kucitanso mantha; koma munalandira mzimu waumwana, umene tipfuula nao, kuti, Abba, Atate, (Aroma 8:15)

ZIZINDIKIRO ZA MZIMU WOYERA

Baibulo limagwiritsa ntchito zizindikiro zingapo zoyimira Mzimu Woyera. Chizindikiro chimayimira chinachake.

Ndichizindikiro chimakhala ndi tanthauzo lapederadera. Zotsatirazi ndi zizindikiro zimene zagwiritsidwa ntchito m’baibulo:

NKHUNDA:

Mzimu Woyera anawonetsedwa mu m’chizindikiro cha nkhunda pamene Yesu amabatizidwa. Chizindikiro chimenechi chimayimira chitsimikizo, chiyero ndi mtendere:

Yohane 1:32 Ndipo Yohane anacita umboni, nati, 8 Ndinaona Mzimu alikutsika kucokera Kumwamba monga nkhunda; nakhalabe pa iye. (John 1:32).

CHITSIMIKIZO:

Ndipo Yohane anacita umboni, nati, 8 Ndinaona Mzimu alikutsika kucokera Kumwamba monga nkhunda; nakhalabe pa iye. (Yohane 1:32)

MTENDERE:

Ndipo ndinati, Ha, wina akadandipatsa mapiko onga a njiwa Mwenzi nditauluka, ndi kukhaliratu. (Masalmo 55:6)

CHIYERO:

Nkhunda yanga, wangwiro wangayunamucha wodala; (Nyimbo 6:9)

MAFUTA:

Mafuta amagwiritsidwa ntchito m'baibulo ngati chizindikiro cha Mzimu Woyera. Mafuta amasonyeza kuwala, machiritso ndi kudzodza kwa utumiki. Zonsezi zimaperekedwa kwa wokhulupirira kudzera mwa Mzimu Woyera.

Mzimu wa Ambuye uli paine, Cifukwa cace iye anandidzoza Ine ndi iye anthu osauka Uthenga Wabwino: Anandituma Ine kulalikira am'nsinga mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyenso, Kuturutsa ndi ufuru ophwanyika, (Luka 4:18)

za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulunguanamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulunguanali pamodzi ndi iye. (Macitidwe 10:38)

Mwakonda cilungamo, ndi kudana naco coipa; Mwa ici Mulungu, ndiye Mulunguwanu, wakudzozani Ndi mafuta a cikondwerero ceni ceni koposa anzanu. (Ahebri 1:9)

MADZI:

Madzi amayimira moyo watsopano ndi kuyeretsedwa ku uchimo kumene Mzimu Woyera amabweretsa kwa munthu wokhulupirira:

Koma tsiku lomariza, lalukurulo la phwando, Yesu anaimirira napfuula, ndi kunena, Ngati pali munthu akumva Ludzu, adze kwa Ine, namwe. Iye wokhulupirira Ine, monga cilembo cinati, Mitsinje ya madzi amoyo idzayenda, kuturuka m'kati mwace. Koma 1 ici anati za Mzimu, amene iwo akukhulupirira iye anati adzalandire; pakuti Mzimu panalibe pamenepo, cifukwa Yesu sanalemekezedwa panthawi pomwepo. glorified. (Yohane 7:37-39)

Pakuti ndidzathira madzi pa dziko limene liribe madzi, ndi mitsinje pa nthaka youma; ndidzathira mzimu wanga pa mbeu yako, ndi mdalitso wanga pa obadwa ako; (Yesaya 44:3)

CHIDINDO:

Chidindo ndi chizindikiro chapaderadera chowonetsa umwini wa chithu. Chimawonetsanso chomwe chachitika. Mzimu Woyera anawayika chizindikiro chimenechi kusonyeza kuti iwo ndi ana a Mulungu. Chimawonetsa chipulumutso chawo ngati ntchito yomwe yachitika pa iwo.

Mwa Iyeyo inunso, mutamva mau a coonadi, Uthenga Wabwino wa cipulumutso canu; ndi kumkhulupirira iye, munasindikizidwa cizindikilo ndi Mzimu Woyera wa lonjezano, (Aefeso 1:13)

Ndipo 10 musamvetse cisoni Mzimu Woyera wa Mulungu, amene munasindikizidwa cizindikilo mwa iye, kufikira tsiku la maomboledwe. (Aefeso 4:30)

**amenenso anatisindikiza cizindikilo, natipatsa cikole ca Mzimu mu mitima yathu. 2
Akorinto 1:22**

MPHEPO:

Mphepo ndi chizindikironso cha Mzimu Woyera. Imayimira mphamvu ya Mzimu Woyera:

Ndipo pakufika tsiku la Penteskoste, anali onse pamodzi pa malo amodzi. Ndipo mwadzidzidzi anamveka mau ocokera Kumwamba ngati mkokomo wa mphepo yolimba, nadzaza nyumba yonse imene analikukhalamo. (Macitidwe 2:1-2)

Mu dziko lachilengedweri sitingathe kuyiwona mphepo, Koma mutha kuwona zizndikiro zosonyeza mphepo. Mu m’dziko lolengedwerari mphepo nili ndi ntchito zapaderadera. Nchito zimenezi zimafanafana ndi ntchito za Mzimu Woyera:

MPHEPO IMABWERETSA MOYO:

Mphepo ikamawomba imamwaza mbewu m’ malo osiyanasiyana, izi zimapangitsa kuti pakhale moyo watsopano. Mzimu Woyera umabweretsa moyo kudzera mu mbewu ya mawu a Mulungu amafesedwa mu mitima ndi m’ malingaliro a anthu. Moyo umenewu simoyo osatha okha ayi komanso moyo wokhwima wa uzimu kudzera m’ chipatso cha mzimu chifukwa cha mbewu ya mawu.

MPHEPO IMASIYANITSA TILIGU NDI MANKHUSU:

Imayeretsa pochotsa zotsalira zilizonse zimene ndizosafunikira pa chinthu. Mzimu Woyera ndimphamvu yoyeretsa m’ moyo wa munthu wokhulupirira.

MPHEPO IMAKUPIZA MALASHA NDIKUWAYATSA MOTO:

Mphepo ya Mzimu Woyera imakupiza anthu a Mulungu kuti atsitsimutsidwe ndi kuwapanga kukhala Malawi a moto wa utumiki ku dziko lapansi.

MOTO:

Moto ndi chizindikiro china cha Mzimu Woyera. Moto umawonetsa izi:

Kupezeka kwa mulungu:

Ndipo mthenga wa Molungu anamuonekera m'cirangali camoto coturuka m'kati mwa citsamba; ndipo anapenya, ndipo taonani, citsamba cirikuyaka moto, koma cosanyeka citsambaco. (Eksodo 3:2)

Chitsimikizo Cha Ambuye:

Ndipo Mose ndi Aroni analowa ku cihema cokomanako, naturuka, nadalitsa anthu; ndipo ulemero wa Yehova unaonekera kwa anthu onse. Ndipo unaturuka mota pamaso ya Yehova, nunyeketsa nsembe yopsereza ndi mafuta pa guwa la nsembe; ndipo pakucionana anthu onse anapfuula, nagwa nkhope zao pansu. (Levitiko 9:23-24)

Chitetezo Ndi Chitsogozo:

Ndipo Yehova anawatsogolera usana ndi mtambo njo kuwatsogolera m'njira; ndi usiku ndi moto njo, wakuwawalitsira; kuti ayende usana ndi usiku; (Eksodo 13:21)

KUYERETSA:

Yesaya 6:1-8 amafotokoza za mneneri Yesaya akuyeretsewa ndi moto wa mzimuwoyera. Werengani ndime imeneyi m'baibulo lanu.

MPHATSO YA MZIMU WOYERA:

Pamene Mzimu Woyera amaperekedwa koyamba, moto unagwiritsidwa ntchito ngatichizindikiro cha kupezeka kwake:

Ndipo anaonekera kwa iwo malilime ogawanikana, onga amoto; ndipo unakhala pa iwo onse wayekha wayekha. (Macitidwe 2:3)

Chiweruzo:

Pakuti 1 Mulunguwathu ndiye mota wonyeketsa. (Ahebri 12:29)

ZOYIMIRA MZIMU WOYERA.

Maina ndi zizindikiro zimene zimayimira Mzimu Woyera zimaulula zolinga zake ndi utumiki. Mautumiki ena owonjezera a Mzimu Woyera afotokozedwa mwatsatanetsatane mu chaputala chomwe chikubwerachi.

MAYESO ODZIYESA NOKHA.

1. Lembani vesi yotsogolera osawonera.

2. Kodi choyimira/chizindikiro ndi chani??

3. Werengami zomwe zimayimira Mzimu Woyera mu mndandanda woyamba. Werengani matanthauzo ake mu mndandanda wachiwiri.

Lembani nambala ya tanthauzo limene likugwirizana kwambiri pa mpata womwe waperekedwa.

Zoyimira Mzimu Woyera.

Mndandanda woyamba Mndandanda wachiwi

- | | |
|--------------|---|
| ____Mphepo | 1.kuyimira chiyero ndi mtendere. |
| ____Chidindo | 2. Kusonyeza kuwala, machiritso ndi kudzodza kwa utumuki. |
| ____Madzi | 3. Kusonyeza moyo ndi kuyeretsa. |
| ____Nkhunda | 4. Kusonyeza umwini wa chinthu. |
| ____Mafuta | 5. Kusonyeza mphamvu. |

4. Moto ndi choyimira cha Mzimu Woyera. Perekani zinthu zisanu ndi m’chimodzi zomwe moto ngati choyimira Mzimu Woyera umatanthauza:

5.Maina khumi ndi atatu a Mzimu Woyera akambidwa mu chaputala chino. Kodi inu ndi angati omwe mungapereke?

(Mayankho a mafunso amenewa aperekedwa kumapeto kwa chaputala chomaliza cha bukuli.)

ZOWONJEZERA POPHUNZIRA

Mu m'chipangano cha tsopano muli ndime zokwana 261 zimene zikukamba za Mzimu Woyera. Iye watchulidwa:

-kokwana 56 mu mabuku amene amakamba za Yesu a Mateyu, Maliko, Luka ndi Yohane.

-kokwana 57 mu buku la Machitidwe.

-kokwana 148 mu mbali yotsala ya chipangano cha tsopano.

Werangani chipangano chose chatsopano. Pamene mukuwerenga muzungulize mawu aliwonse amene akukamba za Mzimu Woyera. Muwerenge ndime zimenezi kuti chidziwitso chanu cha utumiki wa Mzimu Woyera chikule.

CHAPUTALA 3

UTUMIKI WA MZIMU WOYERA

ZOLINGA:

Pomaliza pa phunziroli mukwanitse kuchita izi:

Kufotokozero utumiki wa Mzimu Woyera molingana ndi:

- Chilengedwe
- Mawu a MulunguIsraeli
- Satana
- Yesu
- Munthu wochimwa
- Mpingo
- Okhulupirira

VESI YOTSOGOLERA:

Koma Nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m'dzina langa, 3 Iyeyo adzaphunzitsa Inu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu. (Yohane 14:26)

MAWU OYAMBA

Cholinga cha chaputala ichi ndi kufotokoza za mautumiki a Mzimu Woyera kuyambira pachiyambi pa chilengedwe cha dziko kufikira utumiki wake lero lino kwa okhulupirira.

CHILENGEDWE

Mzimu Woyera analipo pa nthawi ya chilengedwe cha dziko.

**Dziko lapansi ndipo linali lopanda kanthu; ndipo mdima unali pamwamba pa nyanja; ndipo mzimu wa Mulungu unaliokufungatira pamwamba pa madzi.
(Genesis 1:2)**

**Potumizira mzimu wanu, zilengedwa; Ndipo mukonzanso nkhope ya dziko lapansi.
(Masalmo 104:30)**

MAWU A MULUNGU

Utumiki wa Mzimu Woyera umawonekeranso mu mkulembedwa kwa mau a Mulungu kapena kuti Baibulo. Mzimu Woyera anatumikira pa:

VUMBULUTSO:

Iye anayankhula kwa anthu kuti alembe uthenga wa mulungu:

pakuti kale lonse cinenero sicinadza ndi cifuniro ca munthu; koma anthu a Mulungu, ogwidwa ndi Mzimu Woyera, analankhula. (2 Petro 1:21)

KUWUZIRA NDI MPWEYA:

Iye anatsogolera olemba kuti uthenga ukhale opanda zolakwika:

Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitso, citsutsano, cikonzero, cilangizo ca m'cilungamo: kuti munthu wa Mulunguakhale woyenera, wokonzeka kucita nchito iri yonse yabwino. (II Timote 3:16-17)

KUWUNIKIRA:

Iye anawunikira mitima ya anthu kuti amvetsetse uthenga wabwino:

Koma 2 Nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m'dzina langa, 3 Iyeyo adzaphunzitsa Inu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu. (Yohane 14:26).

ISRAELI

Dziko la Israeli linasankhidwa ndi Mulungungati anthu kuti kudzera mwa iwo iye akadziwulule yekha komanso kukwaniritsa cholinga chake chachikulu mu dziko lapansi. Kudzera mwa Israeli Yesu anadza kudzapulutsa anthu ku, machimo.

Zomwe a Israeli amadzutsamo zinapereka chitsanzo cha kupambana ndi kulephera kwa okhulupirira. Kuchokera ku Yerusalemu, likulu la Israeli, uthenga wabwino unafalitsidwa ku dziko lonse lapansi.

Utumiki wa Mzimu Woyera kwa mtundu wa Israeli ukuwonetsedwa kuchokera pachiyambi pomwe. Mzimu Woyera:

ANADZA PA ATSOGOLERI A ISRAELI:

Pali zitsanzo zambiri za izi zomwe ma vesi ake onse sitingathe kuwalemba onse m'bukuli. Mndandanda wa mavesi waperekedwa mu gawo la “zowojezera pophunzira” mu m'chaputalachi. Phunziroli lithandiza kumvetsetsa momwe Mzimu Woyera amagwirira ntchito m'miyoyo ya anthu mu m'chipangano chakale.

ANADZA M'MALO OPEMBEDZERA MU ISRAELI:

Pamenepo mtambo unaphimba cihema cokomanako, ndi ulemerero wa Yehova unadzaza kacisiyo. (Eksodo 40:34)

Ndipo kunacitika ataturuka ansembe m'malo opatulika, mtambo unadzaza nyumba ya Yehova, (1 Mafumu 8:10)

ANAWATSOGOLERA KU DZIKO LA MALONJEZANO:

Munawapatsanso mzimu wanu wokoma kuwalangiza, ndipo simunawamana mana anu pakamwa pao; munawapatsanso madzi pa ludzu lao. (Nehemiya 9:20)

IYE ADZABWERA PA ISRAELI MU NTHAWI YA CHINZUZO CHACHIKULU:

Iyi ndi nthawi yachizuzo chachikulu mtsogolo. Mulunguadzayika chizindikiro cha chitetezochapaderadera pa Israeli.

Ndipo ndinaona mngelo wina, anakwera kucokera poturuka dzuwa, ali naco cizindikilo ca Mulunguwamoyo: ndipo anapfuula ndi mau akuru kuitana angelo anai, amene adalandira mphamvu kuipsa dziko ndi nyanja, nanena, Musaipse dziko, kapena nyanja, kapena mitengo, kufikira tidasindikiza cizindikilo akapolo a Mulunguwathu, pamphumi pao. Ndipo ndinamva ciwerengo ca iwo osindikizidwa cizindikilo, zikwi makumi khumi ndi makumi anai mphambu anai, osindikizidwa cizindikilo mwa mafuko onse a ana a Israyeli, (Cibvumbulutso 7:2-4)

ADZABWERA PA ISRAELI MU NTHAWI YA MILENIYAMU:

Mileniyamu ndi zaka chikwi za mtendere pamene Yesu adzalamulire pa dziko lapansi:

Ndipo ndidzatsanulira pa nyumba ya Davide, ndi pa okhala m'Yerusalemu, mzimu wa cisomo ndi wakupembedza; ndipo adzandipenyera Ine amene anandipyoza; nadzamlira ngati munthu alira mwana wace mmodzi yekha, nadzammvera zowawa mtima, monga munthu amvera zowawa mtima mwana wace woyamba. Zekariya 12:10)

SATANA

Mzimu Woyera ali ndi utumiki wokhudza satana. Mzimu Woyera ali ndi mphamvu za uzimu zakupereka malire kwa satana:

Comweco iwo adzaopa dzina la Yehova kucokera kumadzulo, ndi ulemerero wace kumene kuturukira dzuwa; pakuti pamene mdani adzafika ngati cigumula, mzimu wa Yehova udzamkwezera mbendera yomletsa. (Yesaya 59:19).

Mzimu Woyera akadzachotsedwa ku dziko lapansi, pamenepo mzimu wa wokana khristu adzatenga ulamuliro mwa kanthawi. Wokana khristu adzakhala mtsogoleri wa usatana wa dziko lapansi:

Pakuti cinsinsi ca kusayeruzika cayambadi kucita; cokhaci pali womletsa tsopano, kufikira akamcotsa pakati. Ndipo pamenepo adzabvumbulutsidwa wosayeruzikayo, amene Ambuye Yesu adzamthera ndi mzimu wa pakamwa pace, nadzamuononga ndi maonekedwe a kudza kwace; ndiye amene kudza kwace kuli monga mwa macitidwe a Satana, mu mphamvu yonse, ndi zizindikilo ndi zozizwa zonama; ndi m'cinyengo conse ca cosalungama kwa iwo akuonongeka, popeza cikondi ca coonadi sanacisandira, kuti akapulumsidwe iwo. Ndipo cifukwa cace Mulunguatumiza kwa iwo macitidwe a kusoceretsa, kuti akhulupirire bodza; kuti aweruzidwe onse

**amene sanakhulupirira coonadi, komatu anakondwera ndi cosalungama.
(2 Atesalonika 2:7-12)**

YESU

Utumiki wa Mzimu Woyera unawonetsedwa mu m'moyo wa Yesu:

WOBADWA MWA MZIMU:

Ndipo mngelo anayankha, nati kwa iye, Mzimu Woyera adzafika pa iwe, ndi mphamvu ya Wamkulukulu idzakuphimba iwe: cifukwa cacenso Coyeraco cikadzabadwa, cidzachedwa Mwana wa Mulungu. Luka 1:35

Ndipo kubadwa kwace kwa Yesu Kristu kunali kotere: Amai wace Mariya anapalidwa ubwenzi ndi Yosefe, koma asanakomane iwowo, anapezedwa iye ali ndi pakati mwa Mzimu Woyera. Koma pakusinkhasinkha iye zinthu izi, onani, mngelo wa Ambuye anaonekera kwa iye m'kulota, nanena, Yosefe, mwana wa Davide, usaope kudzitengera wekha Mariya mkazi wako; pakuti ico colandiridwa mwa iye ciri ca Mzimu Woyera. (Mateyu 1:18,20)

ODZODZEDWA NDI MZIMU:

Mzimu wa Ambuye uli paine, Cifukwa cace iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino: Anandituma Ine kulalikira am'nsinga mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyenso, Kuturutsa ndi ufuru ophwanyika, (Luke 4:18)

za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulunguanamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulunguanali pamodzi ndi iye. (Machitidwe 10:38)

Mwakonda cilungamo, ndi kudana naco coipa; Mwa ici Mulungu, ndiye Mulunguwanu, wakudzozani Ndi mafuta a cikondwerero ceni ceni koposa anzanu. (Ahebri 1:9)

WOIKIDWA CHIZINDIKIRO NDI MZIMU:

Gwirani nchito si cifukwa ca cakudya cimene citayika koma ca cakudya cimene citsalira ku moyo wosatha, cimene Mwana wa munthu adzakupatsani inu; pakuti ameneyo Atate, ndiye Mulungu, adamlembera cizindikilo. (Yohane 6:27)

WOTSOGOZEDWA NDI MZIMU:

Pamenepo Yesu anatengedwa ndi Mzimu kumka kucipululu kukayesedwa ndi mdierekezi. (Mateyu 4:1)

WOPATSIDWA MPHAMVU NDI MZIMU:

Koma ngati Ine ndimaturutsa ziwanda ndi mphamvu yace ya Mzimu wa Mulungu, pomwepo Ufumu wa Mulunguunafika pa inu. (Mateyu 12:28)

WODZADZIDWA NDI MZIMU:

Pamenepo Yesu anatengedwa ndi Mzimu kumka kucipululu kukayesedwa ndi mdierekezi. (Mateyu 4:1)

Pakuti 2 Iye amene Mulunguanamtuma alankhula mau a Mulungu; pakuti 3 sapatsa Mzimu ndi muyeso. (Yohane 3:34)

WOVUTITSIDWA MU MTIMA NDI MZIMU:

Pamenepo Yesu, pakumuona iye alikulira, ndi Ayuda akumperekeza iye alikulira, anadzuma mumzimu, nabvutika mwini, (Yohane 11:33)

WOKONDWERA MU MZIMU:

Nthawi yomweyo iye anakondwera ndi Mzimu Wovera, nati, Ndikubvomerezani Inu, Atate, Ambuye wa kumwamba ndi wa dziko, kuti izi munazibisira anzeru ndi ozindikira, ndipo munaziululira ana amakanda; indedi, Atate, pakuti kotero kudakondweretsa pamaso panu. (Luka 10:21)

OPEREKEDWA KUDZERA MWA MZIMU:

koposa kotani nanga mwazi wa Kristu amene anadzipereka yekha wopanda cirema kwa Mulungumwa Mzimu wosatha, udzayeretsa cikumbu mtima canu kucisiyanitsa ndi nchito zakufa, kukatumikira Mulunguwamoyo? (Ahebri 9:14)

WOWUKITSIDWA NDI MZIMU:

1 Petro 3:18 Pakuti Kristunso adamva zowawa kamodzi, cifukwa ca macimo, wolungama m'malo mwa osalungama, kuti akatifikitse kwa Mulungu; wophedwatu m'thupi, koma woparsidwa moyo mumzimu;

amene anatsimikizidwa ndi mphamvu kuti ndiye Mwana wa Mulungumonga mwa Mzimu wa ciyero, ndi kuuka kwa akufa; ndiye Yesu Kristu Ambuye wathu; (Aroma 1:4)

ANALAMULA OPHUNZIRA AKE KUDZERA MWA MZIMU:

kufikira tsiku lija anatengedwa kunka Kumwamba, atatha kulamulira mwa Mzimu Woyera atumwi amene adawasankha; (Macitidwe 1:2)

ANTHU OCHIMWA

Utumiki wa Mzimu Woyera kwa munthu ochimwa unafotokozeredwa ndi Yesu:

Koma ndinena Ine coonadi ndi inu; kuyenera kwa inu kuti ndicoke Ine; pakuti ngati sindicoka, Nkhosweyo sadzadza kwa inu; koma ngati ndipita ndidzamtuma iye kwa inu. Ndipo atadza Iyeyo, adzatsutsa dziko lapansi za macimo, ndi za cilungamo, ndi za ciweruziro; za macimo, cifukwa sakhulupirira Ine; za cilungamo,

cifukwa ndinka kwa Atate, ndipo simundionanso; za ciweruziro, cifukwa mkuru wa dziko ili lapansi waweruzidwa. (Yohane 16:7-11)

MPINGO

Mzimu Woyera amagwira ntchito zosiyanasiyana mu mpingo. Iye...

ANAPANGA MPINGO:

Pamenepo ndipo simulinso alendo ndi ogonera, komatu muli a mudzi womwewo wa oyera mtima ndi a banja la Mulungu; omangika pa maziko a atumwi ndi aneneri, pali Kristu Yesu mwini, mwala wa pangondya; 1 mwa iye cimango conse, columikizika pamodzi bwino, cikula, cikhale 2 kacisi wopatulika mwa Ambuye; 3 cimene inunso mumangidwamo pamodzi, mukhale cokhalamo Mulungumwa Mzimu.

ANAWUZIRA NDI MPWEYA KUPEMBEDZA KWAKE:

pakuti ife ndife mdulidwe, akutumikira popembedza ndi Mzimu wa Mulungu, nadzitamandira mwa Yesu Kristu, osakhulupirira m'thupi (Afilipi 3:3)

AMATSOGOLERA ZOCHITIKA ZA UTUMIKI WAKE:

Ndipo Mzimu anati kwa Filipino, Yandikira, nudziphatike ku gareta uyu. (Macitidwe 8:29)

Ndipo anapita pa dziko la Frugiya ndi Galatiya, atawaletsa Mzimu Woyera kuti asalalikire mau m'Asiya; pamene anafika kundunji kwa Musiya, anayesa kunka ku Bituniya; ndipo Mzimu wa Yesu sanawaloleza; Pamene anaona masomphenyawo, pomwepo tinayesa kuturukirakunka ku Makedoniya, poganizira kuti Mulunguanaitanira ife kulalikira Uthenga Wabwino kwa iwo. (Macitidwe 16:6-7,10)

Ndipo pa kutumikira Ambuye iwowa, ndi kusala cakudya, Mzimu Woyera anati, Mundipatulire Ine Bamaba ndi Saulo ku nchito imene odinawaitanirako. Pamenepo iwo, otumidwa ndi Mzimu Woyera, anatsikira ku Selukeya; ndipo pocokerapo anapita m'ngalawa ku Kupro. (Macitidwe 13:2,4)

AMASANKHA ATUMIKI AKE:

Tadzicenjerani nokha, ndi gulu lonse, pamenepo Mzimu Woyera anakuikani oyang'anira, kuti muwete Eklesia wa Mulungu, umene anaugula ndi mwazi wa iye yekha. (Macitidwe 20:28)

AMADZODZA ALALIKI AKE:

Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m'cionetso ca Mzimu ndi ca mphamvu; (1 Akorinto 2:4)

AMATSOGOLERA ZIGANIZO ZAKE:

Pakuti cinakomer a Mzimu Woyera ndi ife, kuti tisasenzetse inu cothodwetsa cacikuru cina coposa izi zoyenerazi; (Macitidwe 15:28)

AMAWUBATIZA NDI MPHAMVU:

Ndipo pakufika tsiku la Penteskoste, anali onse pamodzi pa malo amodzi. Ndipo mwadzidzidzi anamveka mau ocokera Kumwamba ngati mkokomo wa mphepo yolimba, nadzaza nyumba yonse imene analikukhalamo. Ndipo anaonekera kwa iwo malilime ogawanikana, onga amoto; ndipo unakhala pa iwo onse wayekha wayekha. Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa. (Macitidwe 2:1-4)

OKHULUPIRIRA

Mzimu Woyera amagwira ntchito yofunikira kwambiri mu miyoyo ya okhulupirira. Iye...

AMATSUTSA:

Ndi Mzimu Woyera amene amatsutsa za uchimo kuti awatengere abambo ndi amayi kwa Yesu. Simukadakhala okhulupirira popanda utumiki umenewu wa Mzimu Woyera:

Ndipo atadza Iyeyo, adzatsutsa dziko lapansi za macimo, ndi za cilungamo, ndi za ciweruziro; za macimo, cifukwa sakhulupirira Ine; za cilungamo, cifukwa ndinka kwa Atate, ndipo simundionanso; za ciweruziro, cifukwa mkuru wa dziko ili lapansi waweruzidwa. (Yohane 16:8-11)

AMAMUSINTHA MUNTHU:

Mzimu Woyera amasintho moyo wanu kuti mukhale okhulupirira:

zosati zocokera m'nchito za m'cilungamo, zimene tidazicita ife, komatu monga mwa cifundo cace anatipulumutsa ife, mwa kutsuka kwa kubadwanso ndi makonzedwe a Mzimu Woyera, (Tito 3:5)

Yesu anayankha nati kwa iye, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu. Nikodemoananena kwa iye, Munthu akhoza bwanji kubadwa atakalamba? Kodi akhoza kulowanso m'mimba ya amace ndi kubadwa? Yesu anayankha, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwa madzi ndi Mzimu, sakhoza kulowa ufumu wa Mulungu. Cobadwa m'thupi cikhala thupi, ndipo cobadwa mwa Mzimu, cikhala mzimu. Usadabwe cifukwa ndinati kwa iwe, Uyenera kubadwa mwatsopano. (Yohane 3:3-7)

AMAYERETSA:

Mzimu Woyera amawutenga moyo umene wasinthika ndi chipulumutso ndikubweretsa chikhalidwe chakulungama:

Koma tiyenera ife tiziyamika Mulungunthawi zonse cifukwa: ca inu, abale okonedwa ndi Ambuye, kuti Mulunguanakusankhani inu kuyambira paciyanbi, mulandire cipulumutso mwa ciyeretso ca Mzimu ndi cikhulupiriro ca coonadi; (2 Atesalonika 2:13)

AMABATIZA:

Chaputala 4 cha bukuli chikufotokoza za ubatizo wa Mzimu Woyera:

A Buku Lopatulika 1992 Macitidwe 2:4 Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa. (Acts 2:4)

AMAKHALA MKATI:

Cholinga chokhala mkati ndi chakuti akalimbikitse chilengedwe chatsopano cholandiridwa kudzera mu m'chipulumutso:

Kapena simudziwa kuti thupi lanu liri kacisi wa Mzimu Woyera , amene ali mwa inu, amene muli naye kwa Mulungu? Ndipo simukhala a inu nokha. (1 Akorinto 6:19)

Kodi simudziwa kuti muli Kacisi wa Mulungu, ndi kuti Mzimu wa Mulunguagonera mwa inu? (1 Akorinto 3:16)

Cifukwa cace ngati munthu ali yense ali mwa Kristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano, (2 Akorinto 5:17)

Koma ndinena, Muyendeyende ndi Mzimu, ndipo musafitse cilakolako ca thupi. Pakuti thupi lilakalaka potsutsana naye Mzimu, ndi Mzimu potsutsana nalo thupi; pakuti izi sizilingana; kuti zimene muzifuna musazicite. Ngati Mzimu akutsogolerani, simuli omvera lamulo. (Agalatiya 5:16-18)

Mu m'dziko lino, munthu akakhala m'nyumba mwa kanthawi nyumbayo imaonetsera khalidwe la munthuyo. Chimodzimidzinso, nyumba zathu za uzimu zikuyenera kuwonetsera chikhalidwe cha Mzimu Woyera amene amakhala mwa mkatimo.

KUPATSIDWA MPHAMVU:

kuti monga mwa cuma ca ulemerero wace akulimbikitseni inu ndi mphamvu mwa Mzimu wace, m'kati mwanu. (Aefeso 3:16)

KUBWERETSA UMODZI:

Mzimu Woyera amamulumikiza okhulupirira ndi Mulungukomanso ndi okhulupirira ena. Uwu umatchedwa “umodzi wa mzimu”:

Koma iye wophatikidwa ndi Ambuye ali mzimu umodzi. (I Akorintp 6:17)

Pakuti monga thupi liri limodzi, nilikhala nazo ziwalo zambiri; koma ziwalo zonse za thupilo, pokhala zambiri, ziri thupi limodzi; momwemonso Kristu. Pakutinso mwa Mzimu mmodzi ife tonse rinabatizidwa kulowa m'thupi limodzi, ngakhale Ayuda, ngakhale Ahelene, ngakhale akapolo, ngakhale mfulu; ndipo tonse tinamwetsedwa Mzimu mmodzi. (1 Akorinto 12:12-13)

AMAPEMBEDZERA:

Ndipo momwemonso Mzimu athandiza kufoka kwathu; pakuti cimene tizipempha monga ciyenera, sitidziwa; koma Mzimu mwiniatipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka; (Aroma 8:26)

Koma inu, okonedwa, 3 podzimangirira nokha pa cikhulupiriro canu coyeretsetsa, ndi 4 kupemphera mu Mzimu Woyera, (Yuda 1:20)

mwa pemphero lonse ndi pembedzero mupemphere nthawi yonse mwa Mzimu, ndipo poezera pamenepo cicezerere ndi kupembedzera oyera mtima onse, (Aefeso 6:18)

AMATSOGOLERA:

Koma atadza Iyeyo, Mzimu wa coonadi, adzatsogolera inu m'coonadi conse; pakuti sadzalankhula za iye mwini; koma zinthu ziri zonse adzazimva, adzazilankhula; ndipo zinthu zirinkudza adzakulalikirani. (Yohane 16:13)

kuti coikika cace ca cilamulo cikakwaniridwe mwa ife, amene sitiwendayenda monga mwa thupi, koma monga mwa mzimu. (Aroma 8:4)

AMAWONETSERA CHIKONDI:

Mzimu Woyera amawonetsera chikondi cha khristu kwa okhulupirira komanso kudzera mwa iwo:

ndipo ciyembekezo sicicititsa manyazi; cifukwa cikondi ca Mulungucinatsanulidwa m'mitima mwathu mwa Mzimu Woyera, amene wapatsidwa kwa ife. (Aroma 5:5)

WOFANIZIRA NDI CHITHUZITHUZI CHA KHRISTU:

Mzimu Woyera amawafanizira okhulupirira ndi chithuzithuzi cha khristu:

Koma ife tonse ndi nkhope yosaphimbika popenyenera monga mwa kalirole ulemerero wa Ambuye, tisandulika m'cithunzihunzi comweci kucokera kuulenerero kumka kuulemerero, monga ngati kucokera kwa Ambuye Mzimu. (2 Akorinto 3:18)

AMAVUMBULUTSA CHOWONADI:

Koma kwa ife Mulunguanati onetsera izi mwa Mzimu; pakuti Mzimu asanthula zonse, zakuya za Mulunguzomwe. (1 Akorinto 2:10)

AMAPHUNZITSA:

Ndipo inukudzoza kumene munalandira kucokera kwa iye, kukhala mwa inu, ndipo simusowa kuti wina akuphunzitseni; koma 9 munga kudzoza kwace kukuphunzitsani za zinthu zonse, ndipo kuli koono, sikuli bodza ai, ndipo munga kudaphunzitsa inu, mukhale mwa iye. (1 Yohane 2:27)

AMATSIKIZA CHIPULUMUTSO:

Mzimu yekha acita umboni pamodzi ndi mzimu wathu, kuti tiri ana a Mulungu; (Aroma 8:16)

Ndipo 6 munthu amene asunga malamulo ace akhala mwa iye, ndi iye mwa munthuyo. Ndipo 7 m'menemo tizindikira kuti akhala mwa ife, kucokera mwa Mzimu amene anatipatsa ife. (1 Yohane 3:24)

AMAPEREKA MTENDERE:

Pakuti cilamulo ca mzimu wa moyo mwa Kristu Yesu candimasula ine ku lamulo la ucimo ndi la imfa. (Aroma 8:2)

Koma Ambuye ndiye Mzimuyo; ndipo pamene pali Mzimu wa Ambuye pali ufulu. (2 Akorinto 3:17)

AMATONTHOZA:

ndipo unayenda m'kuopa kwa Ambuye ndi m'cithonhozo ca Mzimu Woyera, nucuruka.... .. (Macitidwe 9:31)

Yohane 14:17,26 ndiye Mzimu wa coonadi; amene dziko lapansi silingathe kumlandira, pakuti silimuona iye, kapena kumzindikira iye. Inu mumzindikira iye; cifukwa akhala ndi inu nadzakhala mwa inu. Koma 2 Nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m'dzina langa, 3 Iyeyo adzaphunzitsa Inu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu. (John 14:17,26)

KUFULUMIZITSA:

Koma ngati Mzimu wa iye amene adaukitsa Yesu kwa akufa akhalabe mwa inu, iye amene adaukitsa Kristu Yesu kwa akufa adzapatsanso moyo matupi anu akufa, mwa Mzimu wace wakukhala mwa inu. (Aroma 8:11)

AMAYANKHULA:

Ndipo pamene adzapita nanu kumlandu, nadzakuperekani, musada nkhawa usanayambe mrandu ndi cimene mudzalankhula; koma ci mene cidzapatsidwa kwa inu m'mphindi yomweyo, mucilankhule; pakuti olankhula si ndinu, koma Mzimu Woyera. (Marko 13:11)

AMAWONETSERA MPHAMVU YA MULUNGU:

Ndipo mau anga ndi kulalikirira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m'cionetso ca Mzimu ndi ca mphamvu; kuti cikhulupiriro canu cisakhale m'nzeru ya anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu. (I Akorinto 2:4-5)

AMAWUZIRA KUPEMBEDZA NDI MPWEYA:

Mulungundiye mzimu; ndipo omlambira iye ayenera kumlambira mumzimu ndi m'coonadi. (Yohane 4:24)

AMAPEREKA MPHAMVU YA KUCHITIRA UMBONI:

Mphamvu ya kuchitira umboni ndi chitsimikizo chenicheni chakuti munthu wabatizidwa ndi Mzimu Woyera.

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. (Macitidwe 1:8)

AMAPEREKA MPHATSO NDI KUWONETSERA (KUKULITSA) CHIPATSO:

Mzimu Woyera amapereka mphatso kwa okhulupirira. Uku ndikuthekera kwa paderadera kuti akwanitse kugwira ntchito moyera ngati mbali imodzi ya mpingo. Mzimu Woyera amawonetsanso chipatso cha mzimu m'moyo wa okhulupirira. Chipatso cha mzimu ndi chikhalidwe cha mzimu m'moyo wa munthu okhulupirira.

Chifukwa cha kufunika kwake, chipatso ndi mphatso za Mzimu Woyera zakambidwa mu machaputala ake.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osawonera.

2. Perekani zolinga zisanu za Mzimu Woyera molingana ndi dziko la Israeli.

3. Kodi mawu awa ndi owona kapena abodza? Mzimu Woyera anagwira nawo ntchito pachilengedwe cha dziko lapansi. Mawuwa ndi: _____

4. Lembani nambala ya tanthauzo loyenera kutsogolo kwa mawu omwe akufotokozeredwa.

Zolinga Za Mzimu Woyera Molingana Ndi Mawu a Mulungu.

_____ Kuwunikira 1. Iye anayankhula kwa anthu olemba uthenga wa Mulungu.

_____ Vumbulutso 2. Utumiki wa Mzimu Woyera tsopano lino umene umathandiza anthu kuti amvetsetse uthenga wabwino.

_____ kuwuzira ndi mpweya 3. Mzimu adatsogolera olemba kuti uthenga ukhale opanda zolakwika

.

5. Perekani vesi yomwe ikufotokoza cholinga cha Mzimu Woyera m'moyo wa munthu wochimwa.

6. Kodi utumiki wa Mzimu Woyera chani molingana satana?

7. Chaputalachi chapereka zolinga khumi ndi chimodzi za Mzimu Woyera m'moyo wa Yesu khristu. Ndi zingati zomwe mungakwanitse kutchula?

8.Chaputalachi chafotokoza zolinga zisanu ndi ziwiri za Mzimu Woyera mu mpingo. Ndizingati zomwe mungakwanitse kutchula?

9. Chaputalachi chafotokoza zolinga makumi aiwiri za Mzimu Woyera m'moyo wa wokhulupirira. Ndizingati zomwe mungathe kutchula?

10.Kodi chizindikiro chenicheni chakubatzidwa ndi Mzimu Woyera chimene chimawoneka m'moyo wa munthu ndi chani?

(Mayankho a mayesowa aperekedwa kumapeto kwa chaputala chomaliza cha bukuli.)

ZOWONJEZERA POPHUNZIRA

1. Werengani ndime za m'baibulo zotsatirazi kuti muphunzire zambiri za utumiki wa Mzimu Woyera ku dziko la Israeli:

Genesis 41:38

Numeri 11:17; 11:25; 27:18

Oweruza 3:10; 6:34; 11:29; 14:6,19; 15:14-15

I Samueli 10:10; 11:6; 16:13

I Mafumu 18:12

II Mafumu 2:15-16

Ezekieli 2:2

Danieli 4:9; 5:11; 6:3

Mika 3:8

II Mbiri 15:1; 24:20

2. Werengani zolinga za Mzimu Woyera m'moyo wa wokhulupirira. Kodi mukumulola Mzimu Woyera kuti agwire ntchito m'magawo amenewa m'moyo wanu?

3. Werengani ma utumiki a Mzimu Woyera ku mpingo. Lingalirani za mpingo womwe inu mumakasonkhana ndi anzanu...Ndi magawo ati amene amalola Mzimu Woyera kuwonetsa zolinga zake? Ndi magawo ati amene akufunika kuwunikira kuti zisinthe?

CHAPUTALA 4

UBATIZO WA MZIMU WOYERA

ZOLINGA ZA PHUNZIROLI:

Pamapeto pa chaputalachi mukwanitse kuchita izi:

- Kupereka tanthauzo la kubatiza.
- Mupeze ma vesi atatu amene akuwonetsera zomwe zidachitika pamene anthu amalandira ubatizo wa Mzimu Woyera.
- Mufotokoze momwe munthu angalandirire ubatizo wa Mzimu Woyera.
- Ntchulani chizindikiro chowonekera cha ubatizo wa Mzimu Woyera.
- Mufotokoze chizindikiro chenicheni cha kubatizidwa ndi Mzimu Woyera.
- Mupereke mndandanda wa momwe munthu angalandirire Mzimu Woyera.
- Landirani ubatizo wa Mzimu Woyera.
- Perekeni zotsutsa zinayi zimene anthu nthawi zina amapereka za ubatizo wa Mzimu Woyera.

VESI YOTSOGOLERA:

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko. (Macitidwe 1:8)

MAWU OYAMBA

Baibulo limakamba za ma ubatizo anayi osiyana:

1. Ubatizo wakumva zowawa womwe Yesu anadutsamo.
2. Ubatizo wa madzi umene yohane m'batizi amachita.
3. Ubatizo wa madzi wachikhristu.
4. Ubatizo wa Mzimu Woyera.

Chaputalachi chakhazikika pa ubatizo wa Mzimu Woyera. (Ma ubatizo ena atatu afotokozeredwa mu phunziro lina la “Harvestime International Institute” mu phunziro la *“Foundations of Faith”*).

TANTHAUZO

Mawu akuti “kubatiza” akutanthauza kuti kumiza motheratu kapena kubisa mu m'chinthu chinachake.

LONJEZO LA UBATIZO

Atauka kwa akufa koma atatsala pang'ono kukwera kumwamba, Yesu anapereka malamulo ofunikira kwambiri kwa omutsatira ake:

Ndipo onani, Ine nditumiza pa inu lonjezano la Atate wanga; koma khalani inu m'mudzi muno, kufikira mwabvekedwa ndi mphamvu yocokera Kumwamba. (Luka 24:49)

Lonjezo lomwe Yesu amanena linali la Mzimu Woyera:

Ndipo Ine ndidzapempha Atate, ndipo adzakupatsani inu Nkhoswe yina, kuti akhale ndi inu ku nthawi yonse, ndiye Mzimu wa coonadi; amene dziko lapansi silingathe kumlandira, pakuti silimuona iye, kapena kumzindikira iye. Inu mumzindikira iye; cifukwa akhala ndi inu nadzakhala mwa inu. Sindidza-kusiyani inu mukhale ana amasiye; ndidza kwa inu. (Yohane 14:16-18)

Ili silinali lonjezo lachilendo. Mphatso ya Mzimu Woyera yakhala ikulonjezedwa kuyambira mu nthawi ya m'chipangano chakale:

Iai, koma ndi anthu a milomo yacilendo, ndi a lilume lina, Iye adzalankhula kwa anthu awa; amene ananena nao, Uku ndi kupuma, mupumitsa wolema, ndi apa ndi potsitsimutsa, koma iwo anakana kumva. (Yesaya 28:11-12)

Sakankhana, ayenda liri lonse m'mopita mwace; akagwa m'zida, siityoka nkondo yao.... (Yoweli 2:8)

Sakankhana, ayenda liri lonse m'mopita mwace; akagwa m'zida, siityoka nkondo yao.

CHIZINDIKIRO CHA MZIMU WOYERA

Monga mwaphunzira mu chaputala chapitachi, Mzimu Woyera ali ndi zolinga zambiri m'moyo wa okhulupirira. Chimodzi mwa zolinga zikuluzikulu ndi kupanga akhristu kuti akhale ochitira umboni amphamvu a uthenga wabwino:

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko. (Macitidwe 1:8)

Chizindikiro chenicheni cha ubatizo wa Mzimu Woyera chinawonekera m'moyo wa mtumwi Petulo. Lisanafike tsiku la pentekoste iye anamukana Yesu kuti samudziwa. Koma iye atabatizidwa ndi Mzimu Woyera anayima ndikupereka umboni wamphamvu wa uthenga wabwino ndipo anthu okwana zikwi zitatatu anatembenuka mtima.

Inali mphamvu ya Mzimu Woyera mu mpingo woyamba yomwe inapangitsa kuti uthenga wabwino ulalikidwe ku dziko lonse lapansi. Buku la Machitidwe limawonetsera za umboni wamphamvu umenewu umene unali chizindikiro cha ubatizo wa Mzimu Woyera.

KUBATIZIDWA NDI MZIMU WOYERA

Pali ndime zisanu ndi ziwiri mu m'chipangano chatsopano zimene mawu akuti “Kubatiza” agwiritsidwa ntchito molingana ndi Mzimu Woyera. Ndime zinayi ndi mawu a Yohane m'batizi mu mabuku a uthenga wabwino wa Yesu khristu:

Inetu ndikubatzani inu ndi madzi kuloza ku kutembenuka mtima; koma Iye wakudza pambuyo panga, ali wakundiposa mphamvu, amene sindiyenera kunyamula nsapato zace: Iyeyu adzakubatzani inu ndi Mzimu Woyera ndi moto: (Mateyu 3:11)

Ndakubatzani inu ndi madzi; koma Iye adzakubatzani ndi Mzimu Woyera. (Marko 1:8 8)

Yohane anayankha, nanena kwa onse, Inetu ndikubatzani inu ndi madzi; koma wakundiposa ine mphamvu alinkudza, amene sindiyenera kumasula lamba la nsapato zace; Iyeyu adzakubatzani inu ndi Mzimu Woyera ndi moto: (Luka 3:16)

Ndipo sindinamdziwa iye, koma wonditumayo kudzabatiza ndi madzi, Iyeyu ananena ndi ine, Amene udzaona Mzimu atsikira, nakhala pa iye, 9 yemweyu ndiye wakubatzani ndi Mzimu Woyera. (Yohane 1:33)

Yesu anayankhula za ubatizo wa Mzimu Woyera:

pakuti Yohane anabatizadi ndi madzi; koma inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera, asanapite masiku ambiri. (Macitidwe 1:5)

Pamene Petulo anayankhula kunyumba kwa Korneliyo anagwiritsa ntchito mawu amene Yesu anayankhula:

Ndipo ndinakumbuka mau a Ambuye, kuti ananena, Yohanetu anabatiza ndi madzi; koma inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera. (Macitidwe 11:16)

Paulo anagwiritsa ntchito mawu akuti “Kubatiza” molingana ndi Mzimu Woyera:

Pakutinso mwa Mzimu mmodzi ife tonse rinabatizidwa kulowa m'thupi limodzi, ngakhale Ayuda, ngakhale Ahelene, ngakhale akapolo, ngakhale mfulu; ndipo tonse tinamwetsedwa Mzimu mmodzi. (1 Akorinto 12:13)

Mawu akuti “kubatizidwa mu” Mzimu Woyera ndi mawu ofanana ndi amene amafotokoza za ubatizo wa chikhristu wa madzi. Mu mbali zonse ziwiri “ubatizo” ndi chitsimikizo chowonekera chotsimikiza cha chinthu cha uzimu chomwe chachitika mkati mwa munthu.

Mzimu Woyera anaperekedwa pa nthawi ya chikondwerere cha Ayuda cha “Pentekosite”. Pachifukwa ichi, kubatizidwa ndi Mzimu Woyera nthawi zambiri umatchedwa kuti “chochitika cha pa pentekosite” ndipo nthawi yoperekedwa kwa mzimu imatchedwa kuti “tsiku la pentekosite”.

Mzimu Woyera anatsika kuchokera kumwamba ndikuwamiza okhulupirira amene anasonkhana m'chipinda chapamwamba ku Yerusalemu. Iwo anakhala akudikira mwachidwi za kubwera kwake popeza Yesu anali atawalonjeza kutero. Petulo ananena kuti chachitikachi ndi kukwaniritsidwa kwa lonjezo la Mulungu,” M’masiku otsiriza... Ndidzathira cha mzimu wanga pa thupi lililonse.” Lonjezo limeneli linaperekedwa ndi mneneri Yoweri:

Ndipo kudzacitika m'tsogolo mwace, ndidzatsanulira mzimu wanga pa anthu onse, ndi ana anu amuna ndi akazi adzanenera, akulu akulu anu adzalota maloto, anyamata anu adzaona masomphenya; ndi pa akapolo ndi adzakazi omwe ndidzatsanulira mzimu wanga masiku awo. (Yoweli 2:28-29)

Amauna ndi akazi, achichepere ndi okalamba amayenere kukhala mgulu la kuthiridwa kwa Mzimu Woyera kumeneku. Amayenera kunenera, kulota maloto ndi kuwona masomphenya. Mzimu wa Mulunguanawadzodza akapolo ndi adzakazi. Pa tsiku lomwe Mzimu Woyera anaperekedwa, Petulo anati:

Koma Petro anati kwa iwo, Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku cikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. Pakuti lonjezano 1 liri kwa inu, ndi kwa ana anu, 2 ndi kwa onse akutali, 3 onse amene Ambuye Mulunguwathu adzaitana. (Macitidwe 2:38-39)

Mawu a Petulo anawulula kuti lonjezo la Mzimu Woyera linali:

-Lonjezo la dziko: "kwa inu" [anthu a chiyuda].

-Lonjezo la banja: "kwa ana anu.”

-Lonjezo la dziko lonse lapansi: "kwa onse amene ali kutali.”

CHIZINDIKIRO CHOWONEKA

Mzimu Woyera samawoneka ndi maso a umunthu. Yesu anafanizira Mzimu Woyera ndi mphepo:

ndipo ndidzagulitsa ana ako amuna ndi akazi m'dzanja la ana a Yuda; ndipo iwo adzawagulitsa kwa anthu a Seba, kwa anthu okhala kutari; pakuti Yehova wanena. (Yoweli 3:8)

Ngakhale kuti mphepo simawoneka, koma zotsatira za mphepo zimatha kuwoneka ndikumveka. Mphepo ikamawomba mfumbi limakwera m'mwamba kuchokera pansu, mitengo imapendamira mbali imodzi, masamba amagwedezeka, mafunde panyanja amadzuka, ndipo mitambo imayendayenda m'mwamba. Zonsezi ndi zizindikiro zowoneka za mphepo. Izi zili choncho ndi Mzimu Woyera. Ngakhale kuti iye samawoneka, zotsatira zimene Mzimu Woyera amatulutsa zitha kuwoneka ndi kumveka.

Pali malo atatu mu m'chipangano chatsopano pamene timawuzidwa zomwe zinachitika anthu atabatizidwa ndi Mzimu Woyera:

1.TSIKU LA PENTEKOSITE:

Machitidwe 2:2-4 ndi tsatanetsatane wa zomwe zidachitika pa tsiku la pentekosite:

Ndipo mwadzidzidzi anamveka mau ocokera Kumwamba ngati m'kokomo wa mphepo yolimba, nadzaza nyumba yonse imene analikukhalamo. Ndipo anaonekera kwa iwo malilime ogawanikana, onga amoto; ndipo unakhala pa iwo onse wayekha wayekha. Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa. (Macitidwe 2:2-4)

2.KUNYUMBA KWA KONELIYO:

Machitidwe 10:44-46 ndi tsatanetsatane wa zomwe zidachitika Petulo atalalikira uthenga wabwino kwa munthu otchedwa Koneliyo ndi banja lake:

Petro ali cilankhulire, Mzimu Woyera anagwa pa onse akumva mauwo. Ndipo 6 anadabwa okhulupirirawo akumdulidwe onse amene anadza ndi Petro, cifukwa pa 7 amitundunso panathiridwa m'phatso ya Mzimu Woyera. Pakuti anawamva iwo alikulankhula ndi malilime, ndi kumkuza Mulungu. Pamenepo Petro anayankha, (Macitidwe 10:44-46)

OTEMBENUKA MTIMA A KU AEFESO:

Machitidwe 19:6 amafotokoza zomwe zidachitika kwa anthu otembenuka mtima oyamba ku Aefeso:

Ndipo pamene Paulo anaika manja ace pa iwo, Mzimu Woyera anadza pa iwo; ndipo analankhula ndi malilime, nanenera. (Macitidwe 19:6)

CHIZINDIKIRO CHA PA ONSEA: MALILIME

Tikamafananitsa ndimezi pali chizindikiro chowonekera chimodzi chomwe chikuwoneka pa onse atatu: Iwo amene anabatizidwa ndi Mzimu Woyera anayankhula ndi malilime. Zizindikiro zina zozwiza za Mzimu Woyera zatchulidwa, koma palibe pa zotchulidwazo zomwe zinawoneka pa zochitika zonse mu ndime zitanu zija.

Pa tsiku la pentekosite kunamveka m'kokomo wa mphepo ndipo panawoneka pa iwo malilime a moto. Izi sizinawoneke pa zochitika zina ziwiri zija. Ku Aefeso otembenuka mtima kumene ananenera. Izi sizinanene kuti zinachikanso pa Tsiku la Pentekosite kapena kunyumba kwa Koneliyo.

Chizindikiro chimodzi chowoneka chomwe atumwi anawona chikuchitika ku nyumba kwa Koneliyondi chakuti anayankhula ndi malilime ena. Chizindikiro chowoneka chimenechi chinali chitsimikizo chakuti banja limeneli labatizidwa ndi Mzimu Woyera. Kuchokera ku ndime za m'baibulozi tikutsimikiza kuti chizindikiro chowonekera choyankhula malilime kudzera mu mphamvu ya Mzimu Woyera chimatsimikiza kuti munthu wabatizidwa ndi Mzimu Woyera.

Chizindikiro cha “malilime” chitha kukhala ziyankhulo zodziwika kwa anthu. Izi ndi zomwe zidachitika pa tsiku la pentekosite:

Ndipo anadabwa onse, nazizwa, nanena, Taonani, awa onse alankhulawa sali Agalileya kodi? ndipo nanga ife timva bwanji, yense m'cilankhulidwe cathu cimene tinabadwa naco? (Macitidwe 2:7-8)

Malilime chithanso kukhala chiyankhulo chosadziwika kwa anthu. Awa amatchedwa kuti malilime osadziwika:

Pakuti iye wakulankhula lilime salankhula ndi anthu, koma ndi Mulungu; pakuti palibemunthu akumva; koma mumzimu alankhula zinsinsi. (1 Akorinto 14:2)

ZOLINGA ZA MALILIME

Chizindikiro cha malilime alandira kudzera mu ubatizo wa Mzimu Woyera ali ndi zolinga zambiri m'miyoyo ya anthu. Werengani 1 Akolinto 14 m'baibulo lanu. Izi ndi zina mwa zolinga za malilimeokhulupirira:

- Kupemphera kwa Mulungu: Vesi 2
- Kudzimangirira wekha: kudzimangirira wekha ndikukulitsa chidziwitso cha uzimu. Vesi 4
- Akamasuliridwa amamangirira mpingo When interpreted they edify the church: Mavesi 12-13
- Kupembedzera: Vesi 14 (Onaninso Aroma 8:26-27)
- Chizindikiro kwa anthu osakhulupirira: Vesi 22
- Kukwaniritsidwa kwa uneneri: Vesi 21 (Onaninso Yesaya 28:11-12)
- Kutamanda: Vesi 15,17

ZOTSUTSA ZA MALILIME

Anthu ena amakana/kuletsa kuyankhula malilime. Izi ndi zina mwa zotsutsa zomwe amanena:

KHRISTU ALIYENSE ALI NDI MZIMU WOYERA:

Chotsutsa chodziwika kwambiri amati m'khristu aliyense amalandira Mzimu Woyera pamene akutembenuka mtima.... Iye samafunikanso chochitikanso china ngati kulandira ubatizo wa Mzimu Woyera.

Koma onani zitsanzo za anthu mu m'chipangano chatsopano amene anali okhulupirira enieni. Atumwi adali atalapa machimo awo ndikukhulupirira kuti Yesu anali Mesiya. Anachitira umboni ndikuvomereza zoonza zake za imfa, kuyikidwa m'manda ndi kuwuka kwake kwa kufa. Yesu anawawuza omutsatira ake:

Ndipo onani Ine nditumiza pa inu lonjezano la Atate wanga; koma khalani inu m'mudzi muno, kufikira mwabvekedwa ndi mphamvu yocokera Kumwamba. (Luka 24:49)

Iye adanenanso kuti:

pakuti Yohane anabatizadi ndi madzi; koma inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera, asanapite masiku ambiri. (Macitidwe 1:5)

Ubatizo wa Mzimu Woyera omwe unalonjezedwa unakwaniritsidwa pa tsiku la pentekoste:

Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa. (Macitidwe 2:4)

Ngakhale kuti atumwi anali kale akhristu komabe mpaka pa tsiku la pentekosite ndi pamene iwo anadzazidwa/kudzidzidwa ndi Mzimu Woyera.

Anthu aku Samalia anamva uthenga wabwino ukulalikidwa. Anakhulupirira ndipo anabatizidwa ndi ubatizo wa madzi, koma sanalandire Mzimu Woyera:

Koma pamene atumwi a ku Yerusalemu anamva kuti Samariya adalandira mau a Mulungu, anawatumizira Petro ndi Yohane; amenewo, m'mene adatsikirako, anawapempherera, kuti alandire Mzimu Woyera: pakuti kufikira pamenepo nkuti asanagwe pa wina mmodzi wa iwo; koma anangobatizidwam'dzina la Ambuye Yesu. Pamenepo anaika manja pa iwo, ndipo analandira Mzimu Woyera. (Macitidwe 8:14-17)

Anthu aku Samalia analandira chipulumutso kudzera mu utumiki wa Filipino. Analandira Mzimu Woyera kudzera mu utumiki wa Petulo Yohane. Kulandira Mzimu Woyera ndi chochitika chosiyana ndi kulandira chipulumutso.

Machitidwe 19:1-6 amafotokoza momwe Paulo anapitira ku mzinda wa Aefeso komwe adakumana ndi anthu omwe amadziwika kuti “ophunzira.” Funso loyamba lomwe Paulo adawafunsa linali loti “kodi munalandira Mzimu Woyera kuyambira nthawi yomwe munakhulupirira”?

Ngati anthuwa adali atalandira Mzimu Woyera pamene amalandira chipulumutso ndiye kuti Paulo sakadafunsa funso limeneri. Chifukwa chakuti Paulo anafunsa limeneri zikutsimikiza kuti anthuwa analandira chipulumutso popanda kubatizidwa ndi Mzimu Woyera. Ngakhale munthu atalandira ubatizo wa Mzimu Woyera pamene iye akutembenuka mtima, komabe ndizosiyana ndi chipulumutso.

Monga mwaphunzira m'mbuyomu, utumiki wa Mzimu Woyera ukuwoneka kuyambira pachilengedwe cha dziko. Chipangano chakale chimayankhula za Mzimu Woyera kuti amabwera pa atsogoleri a uzimu a dziko la Israeli. Mzimu Woyera amagwiranso ntchito mwa anthu ochimwa kuti awabweretse iwo kwa Yesu mkhristu. Koma ma utumiki amenewa a Mzimu Woyera ndi osiyana ndi kubatizidwa ndi Mzimu Woyera. Yesu ananena zimenezi poyera kuti:

ndiye Mzimu wa coonadi; amene dziko lapansi silingathe kumlandira, pakuti silimuona iye, kapena kumzindikira iye. Inu mumzindikira iye; cifukwa akhala ndi inu nadzakhala mwa inu. (Yohane 14:17)

Mzimu Woyera anali ndi ophunzira a Yesu Khristu pa nthawi imeneyo, koma sanali mkati mwawo. Anadzadzidwa (kubatizidwa) ndi Mzimu Woyera pa tsiku la pentekosite.

Mzimu Woyera ali ndi anthu ochimwa kuti awabweretse kwa Yesu mkhristu. Koma izi ndi zosiyana ndi kukhala mkati mwawo.

Mu nthawi ya m'chipangano chakale mphmvu ya Mzimu Woyera imabwera pa atsogoleri a uzimu mu nthawi yapaderadera.

Mu m'chipangano chatsopano Mzimu Woyera anaperekedwa mokhazikika kwa okhulupirira.

Mzimu Woyera anali ndi atsogoleri a uzimu a nthawi ya m'chipangano chakale. Koma sanali mkati mwawo. Uku ndiye kusiyana kwa ma utumiki a Mzimu Woyera mu m'chipangano chakale ndi chipangano chatsopano.

KODI ONSE AMAYANKHULA NDI MALILIME?

Chotsutsa china cha malilime chabwera kudzera mum'kusamvetsetsana za funso la mtumwi Paulo. Pa 2 Akolinto 12:30 akufunsa, “Kodi onse ayankhula ndi malilime?”. Yankho la funso limeneli ndi lakuti “Ayi, onse sayankhula ndi malilime.” Koma Paulo pano sakuyankhula za chochitika cha kubatizidwa ndi Mzimu Woyera. Izi akukamba za mphatso za Mzimu Woyera zimene zitha kugwiritsidwa ntchito ndi anthu okhulupirira.

Koma inundinu thupi la Kristu, ndi ziwalo, yense pa yekha. Ndipotu Mulungu anailea ena m'Eklesia, poyamba arumwi, aciwiri aneneri, acitatu aphunzitsi, pamenepo zozizwa, pomwepo mphatso zamaciritso, mathandizo, maweruziro, malilime a mitundu mitundu. (1 Akorinto 12:27-28 -28)

Paulo akuyankhula za mphatso zimene zitha kugwiritsidwa ntchito ndi anthu a mu mpingo. Mphatso ina ya Mzimu Woyera ndi “malilime a mitundumitundu”. Ndikuthekera kwa paderadera kopereka mauthenga ku mpingo mu m'malilime kudzera mu mphamvu ya Mzimu Woyera.

Ngakhale kuti aliyense akabatizidwa pamawoneka chizindikiro cha malilime, si onse amene amalandira mphatso yapaderadera ya malilime amitundumitundu. {Phunziro limeneli lafotokozeredwa bwino mu chaputala 9}.

MANTHA:

Okhulupirira ena samafunafuna kuti abatizidwe ndi Mzimu Woyera kuwopa kuti akalandira zina osati zochokera kwa mulungu. Koma Baibulo limati:

Koma mwenzi anthu onse akadakhala monga momwe ndiri ine ndekha. Koma munthu yense ali nayo mphatso yace ya iye yekha kwa Mulungu, wina cakuti, wina cakuti. Koma ndinena kwa osakwatira, ndi kwa akazi amasiye, kuti kuli bwino kwa iwo ngati akhala monganso ine. Koma ngati sadziwa kudziletsa, akwatitsidwe; pakuti nkwabwino kukwatira koposa kutentha mtima. Koma okwatitsidwawo ndiwalamulira, si ine ai, koma Ambuye, kuti mkazi asasiye mwamuna, komanso

ngati amsiya akhale osakwatiwa, kapena ayanjanitsidwensho ndi mwamunayo, ndipo mwamuna asalekane naye mkazi. (1 Akorinto 7:7-11)

Pemphani, ndipo cidzapatsidwa kwa inu; funani, ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo cidzatsegulidwa kwa inu; (Mateyu 7:7)

Ngati wokhulupirira apempha chinachake kwa mulungu, monga amachitira Bambo wabwino kuthupi, Mulungusadzalola kuti iye alandire china chilichonse chomwe chitha kumuwononga.

MAIMVAIMVA

Chotsutsa china cha malilime ndi chakuti ndi maimvaimva chabe. Okhulupirira ambiri amene amalandira ubatizo wa Mzimu Woyera amakokomeza maimvaimva awo omwe.

Munthu amakhala ndi maimvaimva mwa chilengedwe. Kutembenukira kwa Yesu Khristu sikumachotsa maimvaimva a munthu. Munthu akatembenuka mtima amamvabe chisoni komanso chimwemwe. Kutembenuka mtima kumamasula maimvaimva a munthu kuti asamatsogozedwe ndi uchimo.

Mawu akuti “chimwemwe” m’ mawu a Mulungu amalumikizana kwambiri ndi Mzimu Woyera. Pa Machitidwe 13:52 timawerenga kuti “ophunzira anadzadzidwa ndi chimwemwe”, komanso ndi Mzimu Woyera. Anthu ena amakhala ndi chimwemwe kwambiri chobwera ndi ubatizo wa Mzimu Woyera kamba kakuti mwachilengedwe maimvaimva awo ndi ochuluka kuposa ena. Amatha kuseka, kukuwa kapena kuchita zinazake zomwe zimawonekera m’ matupi mwao.

Koma maimvaimva amenewa sikuti ndi chizindikiro cha ubatizo wa Mzimu Woyera. Chizindikiro chotsimikiza cha ubatizo wa Mzimu Woyera ndi kuyankhula malilime. Chizindikiro chake ndi mphamvu. Sikuonetsa maimvaimva ngati kuseka, kukuwa, kuvina ndi zina zotero, kumene kumaonetsa munthu kuti wabatizidwa ndi Mzimu Woyera. Mmene munthu amachitira chimwemwe cha Mzimu Woyera akabwera kawirikawiri zomafanana ndi maimvaimva ake a munthuyo.

Koma tisawatsutse amene amawonetsara chimwemwe ndi machitachita ena kamba ka Mzimu Woyera. Baibulo limakamba za anthu amene anali ndi machita atakumana ndi Mulungu mwamphamvu. Anthu anathedwa, kugona panso chafufumimba, kukuwa, kusangalala, ndi kuvina pamanso pa Mulungu. Ndizosangalatsa kuwona machitachita a anthu osiyanasiyana ngati a anthu othamanga. Kufuula, kudumpha ndi kuwonetsa kusangalala kwambiri pa masewero awo. Nanga kuli bwanji kwa ife kuwonetsa kusangalala pa mphatso ya ngati Mzimu Woyera amene amakwaniritsa zolinga zosiyanasiyana m’ miyoyo yathu, amabweretsachimwemwe, komanso kutikonzekeza ndi mphamvu kuti tifikire dziko lonse ndi uthenga wabwino. Olemba buku la masalimo Davite anavomereza. Iye anawonetsera chithunzithunzi za kukondwera, kukweza mawu, machitachita akupembedza Mulungu.

Tiyeni tiyimbire Yehova mokondwera; Tipfuule kwa thanthwe la cipulumutso cathu. Tidze naco ciyamiko pamaso pace, Timpfuulire Iye mokondwera ndi

masalmo. Pakuti Yehova ndiye Mulunguwamkuru; Ndi mfumu yaikuru yoposa milungu yonse. (Masalmo 95:1-3)

Mlemekezeni ndi kulira kwa lipenga; Mlemekezeni ndi cisakasa ndi zeze. Mlemekezeni ndi lingaka ndi kuthira mang'ombe: Mlemekezeni ndi zoyimbira za zingwe ndi citoliro. Mlemekezeni ndi nsanje zomveka: Mlemekezeni ndi nsanje zoliritsa. Zonse zakupuma zilemekeze Yehova. Haleluya. (Masalmo 150:3-6)

Simukuyenera kuchita mantha kuti ubatizo wa Mzimu Woyera upangitsa inu kuchita zinthu zinazake zosalongosoka. Paulo adanena kuti pali nthawi “yakukhala chete” ndi “kudzigwira” pa nkhani yoyankhula malilime (1 Akolinto 14). Iye sakadanena izi zikadakhala kuti Mzimu Woyera amapangitsa kuti asadzigwire. Baibulo limati:

ndipo mizimu ya aneneri imvera aneneri; (1 Akorinto 14:32)

Izi zikutanthauza kuti mphatso iliyonse yomwe Mulungu amapereka imamvera kapena kuti imakhala pansu pa ulamuliro wa iye amene akuyigwiritsa ntchito. Mulungu samachita za chisokonezo popeza....

pakuti Mulungu sali Mulungu wa cisokonezo koma wa mtendere; monga mwa Mipingo yonse ya oyera mtima. (Akorinto 14:33)

Mndandanda uli m'musimu ndi zotsogolera ku ubatizo wa Mzimu Woyera.

LAPANI NDIPO BATIZIDWANI:

Koma Petro anati kwa iwo, Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku cikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. (Macitidwe 2:38)

KHULUPIRIRANI KUTI NDI ZA INU:

Pakuti lonjezano 1 liri kwa inu, ndi kwa ana anu, 2 ndi kwa onse akutali, 3 onse amene Ambuye Mulunguwathu adzaitana... (Macitidwe 2:39)

MUFUNITSITSE (KUFUNITSITSA):

Koma tsiku lomariza, lalikurulo la phwando, Yesu anaimirira napfuula, ndi kunena, Ngati pali munthu akumva Ludzu, adze kwa Ine, namwe. Iye wokhulupirira Ine, monga cilembo cinati, Mitsinje ya madzi amoyo idzayenda, kuturuka m'kati mwace. Koma 1 ici anati za Mzimu, amene iwo akukhulupirira iye anati adzalandire; pakuti Mzimu panalibe pamenepo, cifukwa Yesu sanalemekezedwa panthawi pomwepo. (Yohane 7:37-39)

MUMUVOMEREZE NGATI MPHATSO:

Mzimu Woyera anaperekedwa kale. Anaperekedwa ku mpingo pa tsiku la pentekosite. Chifukwa chakuti iye ndi mphatso, simungachite kalikonse kuti mumulandire:

Koma Petro anati kwa iwo, Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku cikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. Macitidwe 2:38

ici cokha ndifuna kuphunzira kwa inu, Kodi munalandira Mzimuyo ndi nchito za lamulo, kapena ndi kumva kwa cikhulupiriro? Ndipo iye amene akuonjezerani inu Mzimuyo, nacita zimphamvu mwa inu, atero kodi ndi nchito za lamulo, kapena ndi kumva kwa cikhulupiriro? kutidalitso la Abrahamu mwa Yesu Kristu, licitike kwa amitundu; kuti tikalandire lonjezano la Mzimuyo, mwa cikhulupiriro. (Agalatiya 3:2,5,14)

Yambani kukweza ndi kuyamika Mulungu chifukwa cha mphatso ya Mzimu Woyera.

DZIPEREKENI KWA MULUNGU:

Perekani lilime lanu kwa Mulungu pakumkwekweza ndi kupembedza Mulungu. Pamene mukukweza Mulungu mokweza mawu mutha kuyamba kumva ngati chibwibwi m'milomo yanu. Pamene mukupitiriza kupereka lilime lanu kwa Mzimu Woyera iye adzayamba kuyankhula kudzera mwa inu m'mawu achilendo. Ichi ndi zindikiro chowoneka chotsimikiza ubatizo wa Mzimu Woyera:

Iai, koma ndi anthu a milomo yacilendo, ndi a lilume lina, Iye adzalankhula kwa anthu awa; (Yesaya 28:11)

Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa. (Macitidwe 2:4)

KUPEMPHA MAPEMPHERO A OKHULUPIRIRA ENA:

Mzimu Woyera atha kulandiridwa pakusanjikidwa manja. (Machitidwe 8,9,19) kapena opanda kusanjikidwa manja (Machitidwe 2,4,10). Werengani ma chaputala amenewa amene akuwonetsa momwe okhulupirira odzadzidwa ndi Mzimu Woyera angakuthandizireni kubatizidwa ndi Mzimu Woyera.

KUFUNIKA KWA UBATIZO WA MZIMU WOYERA

Ubatizo wa Mzimu Woyera ndi ofunika chifukwa chakuti umapangitsa kuti munthu akhale wochitira umboni wamphamvu wa Uthenga Wabwino:

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko. (Macitidwe 1:8)

Marko 16:17-18 Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzaika manja ao pa odwala, ndipo adzacira. (Mark 16:17-18)

Mzimu Woyera amaperekanso mphatso zapaderadera za mzimu ndi kuwonetsa chipatso cha mzimu m'moyo wanu. Mphatso ndi zipatso ndi phunziro la ma chaputala amene atsala a buku lino.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1.Lembani vesi yotsogolera osawonera.

2.Perekani zotsogolera zisanu ndi chimodzi kuti munthu alandire ubatizo wa Mzimu Woyera.

3.Kodi chizindikiro chowoneka cha ubatizo wa Mzimu Woyera ndi chani?

4.Kodi chizindikiro chenicheni cha ubatizo wa Mzimu Woyera ndi chani? Perekani vesi ya m’baibulo kutsimikiza yankho lanu.

5.Kodi ndi zotsutsa zinayi ziti zimene anthu ena amanena za chizindikiro cha “malilime ena”?

6.Kodi pa zotsutsa zimenezi chilipo chomwe ndi choona molingana ndi mawu a Mulungu?

7.Kodi tanthauzo la “kubatiza?” ndi chani?

8.Perekani ndime zitatu za m’baibulo zomwe zikuwonetsa zomwe zidachitika pamene anthu analandira ubatizo wa Mzimu Woyera.

(Mayankho a mafunsowa aperekedwa kumapeto kwa chaputala chomaliza cha buku lino.)

ZOWONJEZERA POPHUNZIRA

1. Mzimu Woyera watchulidwa kokwana 85 mu nthawi ya m'Chipangano chakale. Mukamawerenga chipangano chakale muzungulize mawu aliwonse amene akutchula Mzimu Woyera. Kuwerenga kumeneku kukuthandizani inu kumvetsetsa utumiki wa Mzimu Woyera isanafike nthawi ya Chipangano cha tsopano. Ngati munamaliza ntchito ngati yomweyi ya m'chipangano chatsopano yomwe munapatsidwa mu chaputala 2, ndiye kuti mukhala ndi kumvetsetsa kokwanira kwa Mzimu Woyera kuchokera m'baibulo lanu.

2. Mzimu Woyera anaperekedwa ngati kukwaniritsa malonjezo amene anaperekedwa mu nthawi ya m'Chipangano chakale. Werengani malonjezo amenewa a Mzimu Woyera:

Chipangano Chakale:

Yesaya 28:11-12

Yoweli 2:28-29

Yesaya 44:3

Chipangano Chatsopano:

Yohane 7:38-39; 14:16-18; 15:26; 16:7-11

Machitidwe 1:4,5,8; 2:38-39

Agalatia 3:14

Luka 24:49

3. Munalandira ubatizo wa Mzimu Woyera? Ngati simunalandire, tsatirani ndondomeko yomwe yaperekedwa mu m'chaputala chino kuti mulandire ubatizowu.

4. Bwerezani kuwerenga zolinga za malilime zomwe zafotokozeredwa mu m'chaputala chino. Ndi ziti mwa zimenezi zomwe mwachitira umboni pakugwiritsa ntchito malilime ena?

5. Bwerezani kuwerenga zotsutsa za kuyankhula malilime zomwe zakambidwa mu chaputala chino. Ganizirani momwe mudzayankhire mukadzamva nthawi ina chimodzi mwa zotsutsanzi chikukambidwa.

CHAPUTALA 5

MPHATSO ZA MZIMU WOYERA

ZOLINGA

Pamapeto pa chaputalachi mukwanitse kuchita izi:

- Kunena tanthauzo la mphatso Mzimu.
- Kupeza komwe mphatsozi zimachokera.
Musiyanitse mphatso za mzimu ndi kuthekera kwachilengedwe.
- Kufotokoza zolinga za mphatso za mzimu.
- Kufotokoza zotsutsa za mphatso za mzimu.
- Kufotokoza momwe mphatsozi zimaperekedwera.
- Kupeza mogwiritsidwe ntchito oipa a mphatso za mzimu.
- Kupeza chifungulo cha kagwiritsidwe ntchito ka mphatso za mzimu.
- Kusiyanitsa mphatso za mzimu zenizeni ndi zonama.

VESI YOTSOGOLERA:

**Koma za mphatso zauzimu, abale, sindifuna kuti mukhale osadziwa.
(1 Akorinto 12:1)**

MAWU OYAMBA

Yesu anasiyira udindo ophunzira ake kuti afalitse uthenga wabwino kufikira dziko lonse lapansi. Mphamvu ya Mzimu Woyera ndi yomwe ikadawathandiza kukwaniritsa ntchitoyi:

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. (Macitidwe 1:8)

Yesu sanangosiya udindo wawukuluwu popanda kuwapatsa kuthekera kuti akwaniritse ntchitoyi. Mphatso za mzimu ndi kuthekera kwa uzimu kopatsidwa ndi Mzimu Woyera kumene kumapereka mphamvu kwa okhulupirira kuti akhale opindula pochitira umboni uthenga wabwino.

Za mphatso za mzimu chinali chiphunzitso chimene Paulo anaphunzitsa ku mpingo woyamba. Iye anati:

**Koma za mphatso zauzimu, abale, sindifuna kuti mukhale osadziwa.
(1 Akorinto 12:1)**

Chaputala chino chabweretsa phunziro la mphatso za mzimu. Machaputala akubwerawa akufotokoza za mphatso zosiyanasiyana za mzimu zimene zimapezeka kwa anthu okhulupirira. Ndongomeko ziperekedwa kuti zikuthandizeni inuyo kuzindikira mphatso zanu za mzimu.

KODI MPHATSO ZA MZIMU NDI CHANI?

Mawu oti “za uzimu” akutanthauza kuti zolamulidwa ndi Mzimu Woyera.” Mpatso ndi chinthu chinachake chopatsidwa kwa munthu kuchokera kwa munthu wina mwa ulele. Mpatso ya mzimu ndikuthekera kwauzimu kopatsidwa kwa munthu okhulupirira ndi Mzimu Woyera kuti atumikire ngati chiwalo cha thupi la khristu.

Pali kusiyana pakati pa “mphatso ya Mzimu Woyera” ndi “mphatso za Mzimu Woyera”. Mpatso ya Mzimu Woyera inachitika pa tsiku la pentekosite (Machitidwe 2) pamene Mzimu Woyera anabwera ngati yankho la lonjezo la Yesu:

Ndipo Ine ndidzapempha Atate, ndipo adzakupatsani inu Nkhoswe yina, kuti akhale ndi inu ku nthawi yonse, ndiye Mzimu wa coonadi; amene dziko lapansi silingathe kumlandira, pakuti silimuona iye, kapena kumzindikira iye. Inu mumzindikira iye; cifukwa akhala ndi inu nadzakhala mwa inu. (Yohane 14:16-17)

“Mpatso ya Mzimu Woyera” inaperekedwa kale ngati yankho la lonjezo.” Mpatso za Mzimu Woyera” ndi kuthekera kwa mzimu komwe Mzimu Woyera amapereka kwa anthu okhulupirira kuti akhale ndikuthekera kokhala ndi utumiki wodlalilika:

Ndipo iwowa anaturuka, nalalikira ponse ponse, ndipo Ambuye anacita nao pamodzi, natsimikiza mau ndi zizindikilo zakutsatapo, Amen. (Marko 16:20)

MPHATSO NDI KUTHEKERA KWA CHILENGEDWE

Pali kusiyana pakati pa mphatso za mzimu ndi kuthekera kwa chilengedwe. Kuthekera kwa chilengedwe ndi kumene munthu amatha kubadwa nako (kuchokera kwa makolo) kapena kuchita kuphunzitsidwa. Mpatso ya mzimu ndikuthekera kwa uzimu kumene munthu sachita kubadwa nako kapena kuphunzitsidwa ndi munthu. Ndikuthekera kwapaderadera kopatsidwa ndi mzimu ndi cholinga chofuna kukwaniritsa zolinga zapaderadera za uzimu.

Ndizotheka kuti kuthekera kwa chilengedwe kutha kuvomerezedwa ndi kudalitsidwa ndi Mzimu Woyera atatembenuka mtima munthu. Chikachitika choterechi kuthekera kwa chilengedwe kuja kumasanduka mphatso komanso kuthekera kwa chilengedwe.

Mwa chitsanzo, munthu atha kukhala ndi kuthekera kolongosola zinthu kamba ka maphunziro amene iye anaphunzira. Atabatizidwa ndi Mzimu Woyera kuthekera kwachilengedwe kumeneku kutha kudalitsidwa ndi Mzimu Woyera ndipo atha kugwiritsidwa ntchito pakulongosola zinthu ngati mphatso ya Mzimu Woyera.

Mpatso za mzimu ndikuthekera kwauzimu kumene kukhala koposa kuthekera kwachilengedwe. Ngakhale kuti tikuyenera kugwiritsa ntchito kuthekera kwachilengedwe komwe tili nako potumikira Mulungu, tikufunikanso kukhala ndi mphatso za mzimu.

ZOLINGA ZA MPHATSO

Zolinga za mphatso za Mzimu Woyera zaperekedwa mu mndandanda pa Aefeso 4:12-15:

kuti akonzere oyera mtima: ku nchito ya utumiki, kumangirira thupi la Kristu; kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa cikhulupiriro, ndi wa cizindikiritso ca Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa cidzaloca Kristu. Kuti tisakhalenso makanda, ogwedezekagwedezeka, natengeka-tengeka ndi mphepo yonse ya ciphunzitsa, ndi tsenga la anthu, ndi kucenjerera kukatsata cinyengo ca kusoceretsa; koma ndi kucita zoonza mwa cikondi tikakule m'zinthu zonse, kufikira iye amene ali mutu ndiye Kristu; (Aefeso 4:12-15)

Molingana ndi ndime imeneyi, zolinga za Mzimu Woyera ndi:

- Kulungamitsa oyera
- Kupititsa patsogolo ntchito ya utumiki
- Kumangirira khristu ndi mpingo

Zolinga za mphatso za mzimu ndi zakuti:

- Tilumikizane (umodzi) mu m'chikhulupiriro.
- Kukula mu m'chidziwitso chatu cha khristu.
- Kukula mu ungwiro, ndi khristu ngati chitsanzo chatu.
- Kukhala okhazikika, osasunthika ndi ziphunzitsa zonama.
- Kukhwima mu mzimu mwa khristu.

UTATU WA MULUNGU NDI MPHATSO

Tinawona m'mbuyomu kuti Mzimu Woyera ndi Mulungu m'modzi mwa atatu wa Mulungu. Mulungu atate, Mulungu mwana ndi Mulungu Mzimu Woyera onse amakhalapo powadzodza okhulupirira ndi mphatso za mzimu:

Ndipo pali mphatso zosiyana, koma Mzimu yemweyo. Ndipo pali mautumiki osiyana, koma Ambuye yemweyo. Ndipo pali macitidwe osiyana, koma Mulunguyemweyo, wakucita zinthu zonse mwa onse. (1 Akorinto 12:4-6)

Mzimu Woyera, Atate ndi Ambuye Yesu Khristu onse atchulidwa mu ndime imeneyi. Kupezeka kwawo pa mphatso za mzimu kwawonetsedwa pa chithunzi chili pansichi:

Vesi 4



Mzimu



Mphatso zosiyanasiyana



(mphatso zosiyana)
(mphatso)

vesi 5



Ambuye



Mautumiki osiyanasiyana



(mautumiki osiyana)

vesi 6



Yehova



Machitidwe osiyanasiyana



(njira zosiyana zakagwiritsidwe ntchito ka

ZIDA ZA UZIMU

Mphatso za mzimu zimaperekedwanso ku mpingo ngati zida za nkondo ya uzimu kuti tikagonjetse mphamvu zauzimu za satana: ²

Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba. (Aefeso 6:12)

Popeza kuti nkondo yomwe anthu okhulupirira amalimbana nawo ndi ya uzimu, zida za uzimu ndi zomwe zimayenera kugwiritsidwa ntchito osati zida zakuthupi. Nthawi zina anthu okhulupirira amalowa mu nkondo ya uzimu imeneyi asakudziwa zida zimenezi. Nthawi zonse munthu akamapita ku nkondo opanda zida, sangayembekezere kuti upambana nkondo. Ichi ndi chifukwa chake tikuyenera kumvetsetsa mphatso za mzimu. Izi ndi mbali imodzi ya zida za uzimu zomwe Mulungu wapereka.

KAGAWIDWE KA MPHATSO

Wokhulupirira aliyense ali ndi mphatso ya mzimu:

Koma kwa yense kwapatsidwa maonekedwe a Mzimu kuti apindule nao. Koma zonse izi acita Mzimu mmodzi yemweyo, nagawira yense payekha monga afuna. (1 Akorinto 12:7,11)

Chifukwa chakuti okhulupirira aliyense ali ndi mphatso ya mzimu, aliyense ali ndi udindo wofufuza kuti apeze ndi kugwiritsa ntchito mphatso zake. Simudzaweruzidwa ndi kuchuluka kwa mphatso zomwe muli nazo. Mudzaweruzidwa pa kukhulupirika kwanu pakagwiritsidwe ntchito ka mphatso zomwe mwapatsidwa. Fanizo la Matalente pa Mateyu 25:14-30 likutsimikiza za

² A Harvestime amapereka phunziro lapadera pa nkondo za uzimu pa mutu wakuti "Nkhondo Yauzimu: Mlozo wa Nkhondo Yauzimu"

choonadi chimenechi. Pali mphatso zambiri za mzimu, koma palibe okhulupirira amene ali ndi mphatso zonse za Mzimu Woyera:

Kodi ali onse atumwi? Ali aneneri onse kodi? Ali aphunzitsi onse? Ali onse ocita zozizwa? Ali nazo mphatso za maciritso onse kodi? Kodi onse alankhula ndi malilime? Kodi onse amasulira mau? (1 Akorinto 12:29-30)

Munthu atha kukhala ndi mphatso zoposera imodzi, koma palibe amene angakhale ndi mphatso zonse za Mzimu Woyera. Zikadakhala choncho ndiye kuti ena sakanafunika mu thupi la khristu.

KUSAGWIRITSA NTCHITO MPHATSO MOYENERA

Mphatso ya mzimu yochokera kwa Mulungu itha kugwiritsidwa ntchito molakwika. Kugwiritsa ntchito molakwika zikutanthauza kuti kugwiritsa ntchito mphatso mosayenera. Mutha kugwiritsa ntchito mphatso za mzimu mosayenera pa:

PAKUSAGWIRITSA NTCHITO MPHATSO ZOMWE MWAPATSIDWA:

Mtumwi Paulo anamuwuzza Timoteo:

Pakuti colengedwa conse ca Mulungu ncabwino, ndipo palibe kanthu kayenera kutayika, ngati kalandiridwa ndi ciyamiko; (1 Timoteo 4:4)

Cifukwa cace ndikukumbutsa iwe ukoleze mphatso ya Mulungu, iri mwa iwe mwa kuika kwa manja anga, (2 Timoteo 1:6)

KUYESA KUGWIRITSA NTCHITO MPHATSO ZOMWE SIZINAPATSIDWE KWA INU:

Pamene Petulo ndi Yohane amatumikira ku Samalia, anakumana ndi munthu dzina lake Simioni amene amafuna atakhala ndi mphatso za mphamvu zomwe iye anawona zikuwonetseredwa. Simioni anapereka ndalama kuti apeze kuthekera kumeneku. Petulo anati:

Koma Petro anati kwa iye, Ndalama yako itayike nawe, cifukwa unalingirira kulandira mphatso ya Mulungu ndi ndalama. Ulibe gawo kapena colandira ndi mau awa; pakuti mtima wako suli wolunjika pamaso pa Mulungu. (Macitidwe 8:20-21)

Mphatso za mzimu zimachokera kwa Mzimu Woyera. Palibe njira ina iliyonse yomwe itha kugwiritsidwa ntchito kuti uzilandire. Sungangoganiza kuti ukhale nazo kapena kugwiritsa ntchito mphatso zina zake za mzimu. Mzimu Woyera ndiye amene ali woyenera kukupatsa iwe. Nthawi ina ana asanu ndi awiri a wamsembe wamkulu anawona zozwizwa za mtumwi Paulo ndipo anayesa kugwiritsa ntchito mphatsoyi kutulutsa ziwanda:

Ndipo unayankha mzimu woipa, nuti kwa iwo, Yesu ndimzindikira, ndi Paulo ndimdziwa, koma inu ndinu ayani? Ndipo munthu, mwa iye amene munali mzimu woipa, anawalumphira nawaposa, nawalaka onse awiriwo, kotero kuti anathawa m'nyumba amarisece ndi olasidwa. (Macitidwe 19:15-16)

Zitha kukhala zoopsa kuyesa kugwiritsa ntchito mphatso popanda kudzodza kwa Mzimu Woyera.

KUSAGWIRITSA NTCHITO BWINO MPHATSO:

Pa I Akolinto 12-14 Paulo akukamba za kugwiritsa ntchito bwino mphatso za mzimu. Mwachidule chiphunzitsa cha machaputala amenewa chikuti:

pakuti Mulungu sali Mulungu wa cisokonezo koma wa mtendere; monga mwa Mipingo yonse ya oyera mtima. Koma zonse zicitike koyenera ndi kolongosoka. (1 Akorinto 14:33,40)

Mulungu siwachisokonezo. Pamene pali chisokonezo mphatso za mzimu sizigwira ntchito bwino. Mphatso za mzimu sizigwira ntchito bwino ngati ukuwapezerera anthu, kupeza chuma, kapena kugwiritsa ntchito mphatso za mzimu pa zikhumbitso zanu zonyasa m'malo moti mutumikire nazo kwa ena.

Ndondomeko ya momwe mungagwiritsire ntchito mphatso za mzimu zomwe Paulo wapereka pa I Akolinto 12-14 zimathandiza kupewa chisokonezo. Mukhala ndi mwayi owerenga izi pa gawo la “zowonjezera pophunzira” mu phunziro lino.

KUKWEZA MPHATSO YANU:

Pamene “mukweza” mphatso yanu, mumayitenga a kuti ndiyapaderadera kuposa mphatso zina. Mumayamba kuyiwona mphatsoyo kuti ndi yayikulu kuposa opereka mphatsoyo.

MPHATSO ZAMBIRI GWERO LIMODZI

Baibulo limawonetsa kuti pali mphatso zambiri zimene zimachokera pa gwero limodzi. Gwero la mphatso za mzimu ndi Mzimu Woyera. Iye amapereka komanso kugwiritsa ntchito mphatsozi m'miyoyo ya anthu okhulupirira:

Ndipo pali mphatso zosiyana, koma Mzimu yemweyo. Ndipo pali mautumiki osiyana, koma Ambuye yemweyo. Ndipo pali macitidwe osiyana, koma Mulunguyemweyo, wakucita zinthu zonse mwa onse. Koma kwa yense kwapatsidwa maonekedwe a Mzimu kuti apindule nao. (Akorinto 12:4-7)

Ndipo pokhala ife ndi mphatso zosiyana, monga mwa cisomo copatsidwa kwa ife, kapena mphatso yakunenera, tinenere monga mwa muyeso wa cikhulupiriro; kapena yakutumikira, tidzipereke ku utumiki uwu; kapena iye wakuphunzitsa, kukuphunzitsako; kapena iye wakudandaulira, kukudandaulirako; wakugawira acite ndi mtima wona; iye wakuweruza, aweruze ndi cangu; iye wakucita cifundo, acite ndi kukondwa mtima. (Aroma 12:6-8)

Pali gwero limodzi la mphatso za mzimu koma pali mphatso zambiri zosiyanasiyana. Palibe mphatso yomwe ndi yoposa inzake. Malo anu mu thupi la khristu zikufanizidwa ndi ziwalo za thupi. Monga momwe lili thupi, ziwalo zing'onozing'ono monga maso zili ntchito yofunika kwambiri, chimodzimodzinso mphatso zowoneka zazing'ono ndizofunika kwambiri

pakayendetsedwe ka mpingo. Mphatso zina zimafuna kuwonetsa udindo wawukulu, koma palibe mphatso yomwe ndiyofunika kwambiri kuposa inzake.

Ziwalo zina za thupi zili ndi udindo wawukulu kuposa ziwalo zina. Mwachitsanzo, diso limathandiza munthu kuwona zomwe zakuzungulira. Limakutsogolera poyenda. Limakuthandiza kuwerenga ndi kuwona ndi kusangalala ndi chilengedwe cha Mulungu. Diso lili ndi udindo wawukulu, koma silofunika kwambiri kuposa chala chachikulu cha kumwendo chomwe chimathandiza kuti munthu aziyenda bwino. Chitsogozo cha diso poyenda chitha kukhala chopanda ntchito popanda kukhala ndi mapazi oyendera. Ntchito ya diso yothandiza kuwerenga itha kukhala yopanda ntchito popanda ubongo umene umathandiza munthu kuti amvetsetse zomwe akuwerengazo. Kusamvana kumabuka mu mpingo ngati anthu ena sakuzindikira mphatso za mzimu za ena kuti ndi mphatso. Mwachitsanzo wina atha kukhala ndi mphatso yakupereka ndipo sangamvetse okhulupirira wina amene amalephera kupereka. Kapena wina atha kukhala ndi mphatso yakuchita zinthu mwadongosolo ndipo iye atha kumadabwa ngakhale kusakondwa kuwona anthu ena akuchita zinthu mosalongosoka.

Okhulupirira aliyense agwiritse ntchito mphatso zake za mzimu pogwira ntchito limodzi ndi okhulupirira ena amene ali ndi mphatso zosiyana. Izi zikachitika, mpingo umagwira bwino ntchito ngati thupi la khristu.

ADINDO A MPHATSO

Inu ndinu adindo okhawo a mphatso za mzimu. Mdindo ndi munthu amene si mwini wake wa chomwe iye akugwirira ntchito. Iye amagwiritsa ntchito chomwe chapatsidwa kwa iye ndi munthu wina. Amagwiritsa ntchito m'malo mwa munthu amene anapereka chinthucho. Ndinu a dindo a Yesu khristu:

Cotero munthu atiyese ife, monga atumiki a Kristu, ndi adindo a zinsisi za Mulungu. (1 Akorinto 4:1)

Mbali ya “zinsisi” zakuti inu ndinu a dindo ndi mphatso za mzimu. Zapatsidwa kwa inu ndi Mzimu Woyera kuti mutumikire Yesu moyenera:

Tiri opusa ife cifukwa ca Kristu, koma muli ocejera inu mwa Kristu; tiri ife ofoka, koma inu amphamvu; inu ndinu olemekezeka, koma ife ndife onyozeka. (1 Akorinto 4:10)

Ngati m'dindo, mudzaweruzidwa pakagwiritsidwe ntchito ka mphatso zomwe mwapatsidwa:

Komatu pano pafunika za adindo, kuti munthu akhale wokhulupirika.

(1 Akorinto 4:2)

MPHATSO ZA MZIMU

Ndime zimene zikukamba za mphatso za mzimu zaperekedwa m'musimu. Werengani ndimezi musanapite ku machaputala akutsogolo. Mavesiwa akupereka mphatso zosiyanasiyana:

-Aroma 12:1-8, I Akorinto 12:1-31

-Aefeso 4:1-16 -I Petro 4:7-11

Kumbukirani kuti mphatsozi ndikuthekera kwa paderadera kochokera kwa Mulungu kuti titumikire mu njira zosiyanasiyana. Kukhala ndi zizindikiro za mphatsozi sizikutanthauza kuti tili ndi mphatso ayi. Mwachitsanzo, okhulupirira onse amayenera kupereka ku ntchito ya Mulungu zopereka ndi zakhumi. Koma mphatso yakupereka kolowa manja ndi kosiyana ndi kupereka wamba chifukwa kupereka ngati mphatso kumachitika ndi mzimu wa Mulungu. Okhulupirira onse ali ndi mulingo wa chikhulupiriro molingana ndi mawu a Mulungu. Koma mphatso ya chikhulupiriro ndi kuthekera kwa paderadera kokhulupirira kuposera akhristu ena amene alibe mphatsoyi.

KODI MPHATSO NDI ZA LERO LINO?

Anthu ena amanena kuti mphatso zonse zomwe zaperekedwa mu Baibulo si zampingo wa lero ayi. Amakhulupirira kuti mphatso zina monga uneneri, malilime ndi zozwizwa zinali za mpingo woyamba basi. Anthu amenewa amanena kuti mpingo utakhazikika komanso Chipangano chatsopano chitalembedwa, mphatso zina za mzimu sizimafunikanso ayi. Anthu amenewa amagwiritsa ntchito 1 Akolinto 13:10 pofotokozera chikhulupiriro chawochi.

Koma pamene cangwiro cafika, tsono camderamdera cidzakhhalacabe. (1 Akorinto 13:10)

Iwo amanena kuti pamene vumbulutso langwiro la mau a Mulungu linalembedwa, panalibeso kufunika kwa malilime, kumasulira ndi uneneri. Iwo amanena kuti pamene mpingo unakhazikidwa panalibenso kufunika kwa zozwizwa ndi zodabwitsa ngati chitsimikizo:

Cikondi sicitha nthawizonse, koma kapena zonenera zidzakhala cabe, kapena malilime adzaleka, kapena nzeru idzakhala cabe. (1 Akorinto 13:8)

Ngati tingagwiritse ntchito vesi limeneli kuti malilime, kumasulira ndi uneneri sizikufunikanso, ndiye kuti tikuyenera kunenanso kuti chidziwitso sichikufunikanso. Ndime imeneyi makamaka ikukamba za nthawi ya mtsogolo pamene ufumu wa mgwiro wa Mulungu udzadza kudzakhazikitsidwa pa dziko lapansi. Popeza kuti cha mgwiro chabwera, sitidzafunikiranso mphatso ya mzimu iliyonse chifukwa chakuti...

Ndipo ndinamva mau akuru ocokera ku mpando wacifumu, ndi kunena Taonani, cihema ca Mulunguciri mwa anthu; ndipo adzakhallitsa nao, ndi iwo adzakhala anthu ace, ndi Mulunguyekha adzakhala nao, Mulunguwao; (Cibvumbulutso 21:3)

Sitidzafunanso mauthenga kudzera mu uneneri, m'malilime kapena kumasulira, pakuti tizidzakhala ndi Mulungu amene amadzodza mauthenga ngati amenewo. Sitidzafunanso mawu a

nzeru, popeza tizidzakhala ndi iye amepereka nzeru. Sitidzafunanso chidziwitso cha mizimu, kamba kakuti...

ndipo simudzalowa konse momwemo kanthu kali konse kosapatulidwa kapena iye wakucita conyansa ndi bodza; koma iwo okha olembedwa 7 m'buku la moyo la Mwanawankhosa. (Cibvumbulutso 21:27)

Sipadzafunikanso mphatso ya machiritso kamba ka kuti...

Pakati pa khwalala lace, ndi tsidya ili la mtsinje, ndi tsidya lace lija panali mtengo wa moyo wakubala zipatso khumi ndi ziwiri, ndi kupatsa zipatso zace mwezi ndi mwezi; ndipo masamba a mtengo ndiwo akuciritsa nao amitundu. (... Cibvumbulutso 22:2)

Komanso kumbukirani zolinga za mphatso za mzimu zomwe zaperekedwa pa Aefeso 4:12-15. Zolinga zake ndi kuti:

- Kubweretsa ungwiro kwa oyera mtima.
- Kupititsa patsogolo ntchito ya utumiki.
- Kumangirira khristu ndi mpingo.

Zolinga zimene mphatso za mzimu zinaperekedwera zilipobe. Oyera mtima akufunikirabe kulungamitsidwa, utumiki ukufunikirabe kupita patsogolo kufikira kumalekezere a dziko lapansi, ndipo akhristu ndi mpingo zikufunikabe kumangirirdwa

Zolinga ndi zakuti ife:

- Tidzakhale pa umodzi m'chikhulupiriro.
- Tidzakule m'chidziwitso cha khristu.
- Kuwonetsera ungwiro, ndi khristu ngati chitsanzo chathu.
- Tidzakhale olimba osagwedezeka, osanamizidwa ndi ziphunzitso zonama.
- Okhwima mu mzimu mwa khristu.

Mulungu sakanapereka mphatso za mzimu pa zolinga zimenezi ndikuzichotsanso zolingazo zisanakwaniritsidwe.

- Kodi okhulupirira onse ndi olumikizana mu mzimu?
- Kodi aliyense wakhazikika kwa thunthu mu m'chidziwitso cha khristu?
- Kodi tonse talungamitsidwa?
- Kodi ma membala a mpingo wathu akhazikika kuti sanganamizidwe ndi ziphunzitso zonama?
- Kodi ma membala onse a mpingo ndi okhwima mu mzimu?

Yankho ku mafunso onsewa ndi lakuti “ayi”. Zolinga zimenezi sizinakwaniritsidwe. Pachifukwa chimenechi tikudziwa kuti mphatso za mzimu zikufunikabe lero lino. Mulungu anapereka mphatso za mzimu kuti akwaniritse zolinga zinazake mu mpingo. Iye sadzachotsa mphatso iliyonse zolingazi zake zisanakwaniritsidwe. Baibulo limanenanso kuti “mphatso ndi maitanidwe a Mulungu ndi osalapika” (Aroma 11:29). Izi zikutanthauza kuti Mulungu sadzasintha malingaliro ake ndikutenga mphatso ya mzimu kapena mayitanidwe amene iye wapereka.

CHIFUNGULO CHAKAGWIRITSIDWE KA MPHATSO

Pa I Akolinto 13 Mtumwi Paulo akupereka chifungulo chakagwiritsidwe ntchito ka mphatso za Mzimu Woyera. Iye anabweretsa phunziroli pa I Akolinto 12:31. Iye anapereka mndandanda wa zina mwa mphatso za Mzimu Woyera ndipo anati...

**Koma funitsitsani mphatso zoposa. Ndipo ndikuonetsani njira yokoma yoposatu.
(1 Akorinto 12:31)**

Pa I Akolinto chaputala 13 amafotokoza za “njira ya bwino kopambana”. Werengani chaputalachi panokha m’baibulo lanu. Chaputalachi chikupereka chifungulo chakagwiritsidwe ntchito ka mphatso za mzimu. Chifungulo ndi chikondi. Mutha kunenera, kukhala ndi mphatso ya machiritso, chikhulupiriro, kupereka ndi zina zotero, koma popanda chikondi pakagwiritsidwe ntchito ka mphatso, sizidzapindula.

Mphatso zimakhala zopanda phindu zikamagwiritsidwa ntchito popanda chikondi. Kuyankhula m’malilime kumakhala ngati phokoso. Mphatso iliyonse ndiyopanda pake,” sipindula kanthu”, ngati sikugwiritsidwa ntchito ndi chikondi. Chikondi ndiyo “njira yabwino kwambiri” ya momwe mphatso zikuyenera kugwiritsidwa ntchito. Mphatso zimakhala njira zimene chikondi cha Mulungu chimayenda motizungulira. Chikondi ndi chifungulo chakagwiritsidwe ka mphatso modalirika.

CHENJEZOA: ACHINYENGO A SATANA

Satana amasandutsa mphatso za Mzimu Woyera kukhala za chinyengo. Chinthu chonyenga ndi chomwe chimawoneka ngati chenichenicho, koma sichimakhala chenicheni ayi. Satana ndi onyenga. Baibulo limanena kuti iye nthawi zina amawoneka ngati mngero wakuwunika (2 Akolinto 11:14). Mmasiku otsiriza, kudzakhala khristu onyenga wotchedwa wokana khristu (1 Yohane 2:18,22).

Mphatso zambiri zonyenga zimakwaniritsidwa ndi amatsenga. Mwachitsanzo, mawu anzeru achinyengo amanenedwa ndi asing’anga ponamizira kunenera za m’tsogolo ndi zina zosadziwika ndi anthu. Msing’anga ndi munthu amene amafunafuna kuchita zinthu zodabwitsa ndi zozizwa koma zosachokera kwa Mulungu. Iwo amazitenga kwa satana. Mzimu wachidziwitso wonyenga umachitika ndi anthu amene amatha kudziwa malingaliro a munthu. Ngakhale zozizwitsa zonyenga (Eksodo 7) zizidzachitika ndi okana khristu (Chivumbulutso 13:14). Baibulo limakambanso za aneneri onyenga (Machitidwe 13:6-12). Funso ndi lakuti ,kodi mumasiyanitsa bwanji chenicheni ndi chonyenga?. Chonyenga sichimakwaniritsa cholimba cha chamawu a

Mulungu pa mphatso za Mzimu Woyera .Werenganinso Aefeso 4:12-15.Mphatso iliyonse ya Mzimu Woyera imakwaniritsa zolinga za uzimu zimenezi.Zonyenga sizimagwirizana ndi zimene baibulo limaphunzitsa za Yesu khristu. Kodi munthu akamatumikira mphatso, amati chiani za Yesu? Kodi zimagwirizana ndi mawu olembedwa a mulungu?

Koma ndiopa, kuti pena, monga njoka inanyenga Heva ndi kucenjerera kwace, maganizo anu angaipsidwe kusiyana nako kuona mtima ndi kuyera mtima ziri kwa Kristu. Pakutitu ngati iye wakudza alalikira Yesu wina, amene ife sitinalalikira, kapena ngati mulandira mzimu wa mtundu wina, umene simunalandira, kapena uthenga wabwino wa mtundu wina umene simunalandira, mulolana nave bwino lomwe. (2 Akorinto 11:3-4)

Muthanso kuzindikira onyengawa pakuwona zomwe iwo amachita (makhalidwe awo). Mndandanda wa zimenezi waperekedwa pa 2 Petro 2 komanso m’buku la Yuda.Werengani zimenezi m’baibulo lanu kuti zikuthandizeni kusiyanyitsa pakati pa onyenga ndi enieni.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1.Lembani vesi yotsogolera osawonera

2.Kodi mphatso za Mzimu Woyera zimasiyana bwanji ndi kuthekera kwa munthu kwa chibadwidwe (Talenti)?

3. Perekani ntchito zitatu za Mzimu Woyera:

4. Perekani zolinga zisanu za mphatso za Mzimu Woyera zi:

5. Kodi aliyense alinayo mphatso ya Mzimu Woyera? Perekani ndime ya m’baibulo pofuna kutsimikiza yankho lanu.

6. Perekani njira zinayi zosonyeza kusagwiritsa ntchito bwino mphatso za mzimu:

7.Kodi mphatso za mzimu zimachokera kuti? _____

8.Kodi chifungulo chakagwiritsidwe ntchito ka mphatso yanu ya mzimu ndi chiyani?

9.Kodi mungasiyanitse bwanji mphatso zenizeni za Mzimu Woyera ndi zonyenga za satana?

10.Kodi mphatso za mzimu ndi chiyani?

11.Kodi mphatso zonse za mzimu zikufunikabe lero lino, kapena zina zinali za mpingo woyamba wokha? Fotokozani yankho lanu.

12. Kodi pali kusiyana kotani pakati pa “mphatso za mzimu” ndi “mphatso ya Mzimu Woyera ”?

13. Werengani chiganizo chilichonse. Ngati chiganizocho chili choona lembani T pa mpata womwe uli koyambirira kwa chiganizocho. Ngati chiganizocho chili chabodza lembani F pa mpata umene uli koyambirira kwa chiganizocho.

- a. _____ Kuthekera kwa chilengedwe kochita zinthu si mphatso za Mzimu Woyera.
- b. _____ Munthu amabadwa ndi mphatso za mzimu.
- c. _____ Mulungu amapereka mphatso za mzimu makamaka kuti zikhale zonyaditsa.
- d. _____ Pakuti mpingo ndi wokhazikika kwambiri, zizindikiro zodabwitsa za mphamvu ya Mulungu sizikufunikanso lero lino.
- e. _____ "Chimene chili changwiro chilipo kale lero lino, choncho sitikufunikanso malilime, chimasuliro ndi uneneri.
- f. _____ Palibe mkhristu amene ali ndi mphatso zonse.
- g. _____ Sitingathe kusankha mphatso zathu.
- h. _____ Tidzayankha pamanso pa Mulungu za momwe timagwiritsira ntchito mphatso zathu.
- i. _____ Mphatso zomwe zimagwiritsidwa ntchito popanda chikondi zilibe phindu.

(Mayankho a mafunso amenewa aperekedwa kumapeto kwa chaputala chomaliza cha buku lino.)

ZOWONJEZERA POPHUNZIRA

1. Werengani II Petero 2 komanso buku la Yuda. Perekani makhalidwe a “aneneri onyenga” ndi “amuna ena amene amakwawira mosadziwika”. Awa ndi anthu achinyengo. Awa si ohkulupirira enieni ndipo amagwiritsa ntchito mphatso zoyenga kuti anyenge anthu a Mulungu.

2. Kuthekera kwa chilengedwe kochita zinthu kutha kugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu ngati mphatso za mzimu.

Onani mavesi awa. Perekani mndandanda wa maina a anthu ndi kuthekera kwawo kwa chilengedwe kochita zinthu:

KUTHEKERA KWA CHILENGEDWE KOCHITA ZINTHU (MATALENTE)

Ndime	Dzina	Talente
Genesis 4:20	_____	_____
Genesis 4:2	_____	_____
Genesis 4:21	_____	_____
Genesis 4:22	_____	_____
Genesis 25:27	_____	_____

3. Werengani ndime zotsatirazi ndipo muyike mayankho mu mipata am’ziganizo zomwe zili m’musimu.

Ndizofunika kudziwa za mphatso za mzimu chifukwa chakuti:

a. Tidzayenera _____ kwa Mulunguza momwe tagwiritsira ntchito.

Ife ndife _____.

(I Peturo 4:10; I Akolinto 4:1-2; Mateyu 25:14-30)

b. Tikuyenera kukhala _____.

(I Timoteyo 4:14; I Akolinto 12:1)

4. I Akolinto 13 akupereka mndandanda wa kuposa kwa chikondi. Lembani nambala ya vesi limene likutchula kuposa kwa chikondi mu mipata yomwe mwapatsidwa:

__5__ Chimapirira

_____ chifundo

_____ chopanda nsanje

_____ chosadzitamandira

_____ chilibe mwano

- _____ sichimafuna za icho chokha
- _____ sichikwiya
- _____ sichimasunga mangawa, chimapirira
- _____ sichikondwera ndi chosalungama
- _____ chikondwera ndi choonadi
- _____ chinyamula zinthu zonse
- _____ chimakhulupirira zinthu zonse
- _____ chiyembekeza mu zinthu zonse
- _____ chimapirira zinthu zonse

Lembani dzina la munthu amene sumamukonda. Onaniso kuposa kwa chikondi mu mndandanda uli pamwambawu. Perekani kuposa kwa chikondi kumene mukufuna kuti munthu ameneyu muzimukonda.

Sindimukonda _____.

5. Gwiritsani ntchito mndandanda otsatirawu kuti muwerenge za kagwiritsidwe ntchito kabwino ka mphatso komwe kafotokozeredwa ndi Paulo pa 1 Akolinto 12-14.

I. Mukuyenera kukhala ndi chidziwitso cha mphatso za uzimu: 1 Akolinto 12:1

II. Pali mphatso zambiri koma zonse zimachokera kwa mzimu m' modzi: Utatu wa Mulungu ukugwira ntchito mu mphatso zonse. 1 Akolinto 12:4-11

III. Tikuyenera kugwira ntchito ngati thupi limodzi pogwiritsa ntchito mphatso za Mzimu Woyera: Chiwalo chilichonse chikhale cholera ndi ziwalo zinzake. 1 Akolinto 12:12-31.

A. Pasakhale kugawikana mu m'thupi. Tonse tisamalane wina ndi nzake: 1 Akolinto 12:25-26.

B. Mulungu anayika mphatso mwandondomeko mu mpingo: 1 Akolinto 12:28.

C. Aliyense ali ndi mphatso yosiyana ndi nzake: 1 Akolinto 12:28-30.

D. Tifunefune mphatso za mzimu. 1 Akolinto 12:31; 14:1.

E. Chikondi ndi chifungulo chakagwiritsidwe ntchito ka mphatso zonse: 1 Akolinto 13.

F. Mphatso zimangilire mpingo: I Akolinto 14:12

IV. Ngati muli ndi mphatso ya malilime mupempherenso mphatso yomasulira malilime: I Akolinto 14:1-13

A. Kumukweza Mulungu mu mzimu ndi kumukweza Mulungu ndi chidziwitso zonsenzi ndi mbali za kulambira Mulungu: 1 Akolinto 14:14-15

B. Kuyankhula mawu omveka pamene pali anthu osakhulupirira Mulungu ndi kofunika: I Akolinto 14:16-19

C. Malilime ndi chizindikiro cha kwa iwo osakhulupirira Mulungu: I Akolinto 14:22-25

D. Kunenera kumapindulira iwo akukhulupirira: I Akolinto 14:22-25

V. Zonse zichitike mwadongosolo mu nthawi ya mapemphero. Malilime asachitike pokhapokha pakhale wina amene ali ndi mphatso yomasulira malilime:

I Akolinto 14:26-31

A. Sumalephera kudzigwira pamene Mzimu Woyera akutumikira kudzera mwa inu. Muli ndikuthekera kodzigwira (kolamulira) pakagwiritsidwe ntchito ka mphatso za Mzimu moyenera: I Akolinto 14:32

B. Mulungu si Mulungu wa chisokonezo: I Akolinto 14:33

VI. Musaletse kuyankhula malilime ndipo mufunefune kunenera: I Akolinto 14:39

VII. Mafunso opusa asakhale gawo limodzi la mwambo wopembedza mulungu: I Akolinto 14:34-35,37-38

VIII. Langizo lalikulu lakagwiritsidwe ntchito ka mphatso za mzimu: Zinthu zichitike mwadongosolo ndi moyenera. I Akolinto 14:40

CHAPUTALA 6

MPHATSO ZAPADERADERA ZA MZIMU WOYERA

ZOLINGA ZA PHUNZIRORI:

Pamapeto pa phunziro mukwanitse kuchita izi:

- Mutchule magawo anayi a mphatso za mzimu amene agwiritsidwa ntchito mu m'phunziro lino.
- Mupeze mphatso zapaderadera za Mzimu Woyera.
- Mufotokoze kusiyana kwa mphatso yapaderadera ya kukhala ya mneneri ndi mphatso ya uneneli.
- Mufotokoze kusiyana kwa mphatso yapaderadera ya kukhala m'phunzitsi ndi mphatso ya uphunzitsi.

VESI YOTSOGOLERA:

Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; (Aefeso 4:11)

MAWU OYAMBA

Musanayambe kuphunzira chaputala chino werengani ndime za Baibulo zomwe zili pamunsipa. Ndimezi zikupereka mndandanda wa mphatso za Mzimu Woyera:

-Aroma 12:1-8

-I Akorinto 12:1-31

-Aefeso 4:1-16

-I Petro 4:7-11

Pitani ku gawo la “zakumapeto” kwa bukuli. Werengani ndime zomwezi zimene zatambasulidwa mu Baibulo la “Amplified”. Kuti muphunzire bwino, tagawa mphatso mu magawo anayi akuluakulu:

-Mphatso zapaderadera

-Mphatso zoyankhula

-Mphatso zotumikira

-Mphatso za zizindikiro

Baibulo silimagawa mphatsozi motero. Izi tapanga kuti zikuthandizeni inu kukumbukira mosavuta mphatso zosiyanasiyana. Chaputalachi chikukamba za mphatso zapaderadera. Machaputala otsatirawa akukamba za mphatso zotumikira, mphatso zotumikira ndi mphatso zazizindikiro.

ZOYIKIDWA MU M'THUPI

Chaputala chapitachi chimafotokoza za umodzi wa mphatso zosiyanasiyana za mzimu. Ngakhale kuti pali mphatso zosiyanasiyana koma zonse zimachokera kwa mzimu m' modzi. Opereka zonse ndi Mzimu Woyera. Mulungu ali ndi malo akeake mu mpingo a munthu wina aliyense:

**Koma tsopano, Mulunguanaika ziwalo zonsezo m'thupi, monga anafuna.
(1 Akorinto 12:18)**

Aliyense ali ndi malo amene Mulungu wamusankhira iye. Amakonzeretsedwa kuti akwaniritse cholinga chake chapaderadera mu mpingo kudzera mu mphatso za Mzimu Woyera.

Pamene okhulupirira aliyense akukwaniritsa malo amene Mulungu adamusankhira ndikugwiritsa ntchito mphatso zake za mzimu, mpingo umayenda bwino. Mulungu akuyerekezera ndi thupi la munthu momwe limagwirira ntchito pamene chiwalo chilichonse chimagwira ntchito yake.... kuyambira maso mphaka ku chala chachikulu cha kuphanzi. Chilichonse chimadziwa ntchito yake ndipo chimagwira ntchitoyo. (1 Akolinto 12:1-31).

Kumbukirani pamene mukuphunzira chaputala chino kuti mphatso iliyonse ndi yofunika mofanana mu m'thupi la khristu monga chiwalo chilichonse chili chofunika mu m'thupi la munthu:

Ndipo dise silingathe kunena kwa dzanja, Sindikufuna iwe, kapenanso mutu kwa mapazi, Sindikufunani inu. Koma makamakatu ziwalozo zoyesedwa zofoka m'thupi, zifunika; (1 Akorinto 12:21-22)

Kumbukiraninso kuti mphatso za Mzimu Woyera si kuthekera kwa chilengedwe. Kumeneku ndikuthekera kochokera kwa Mzimu Woyera kowakonzekeretsa okhulupirira ku utumiki wa chikhristu.

(Dziwani izi: Mu m'chaputala chino komanso machaputala atatu otsatirawa paperekedwa njira “zowonjera pophunzira” pamene mphatso iliyonse ya mzimu ikufotokozeredwa. Izi zili choncho kuti zikuloleni inu kumaliza phunziro lanu la mphatso iliyonse musanapite ku chaputala china.

MPHATSO ZAPADERADERA

Gulu loyamba la mphatso za mzimu ndi limene tikulitcha kuti “mphatso zapaderadera”. Timagwiritsa ntchito mutu umenewu chifukwa chakuti mphatso zimenezi iliyonse ili ndi utsogoleri wapaderadera mu mpingo:

Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; (Aefeso 4:11)

Maudindo a utsogoleri amenewa nthawi zina amatchedwa kuti “Ma ofesi” amumpingo. Mawu oti “Ofesi” amatanthauza kuti malo a udindo. Mphatso zapaderadera za utsogoleri ndi izi:

-Atumwi

-Aneneri

- Alaliki
- Abusa
- Aphunzitsi

ATUMWI

Ndipotu Mulungwanailea ena m'Eklesia, poyamba atumwi, aciwiri aneneri, acitatu aphunzitsi, pamenepo zozizwa, pomwepo mphatso zamaciritso, mathandizo, maweruziro, malilime a mitundu mitundu. (1 Akorinto 12:28)

Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; (Aefeso 4:11)

Mtumwi ndi munthu amene ali ndi kuthekera kwapaderadera kodzala mipingo yatsopano mmalo osiyanasiyana a anthu azikhalidwe zosiyanasiyana ndi kumayang'anira mipingo ingapo ngati oyang'anira wamkulu. Mtumwi ndi munthu otumidwa ndi mphamvu komanso ulamuliro kuti akagwire ntchito mmalo mwa wina. Mtumwi ali ndi kuthekera komanso ulamuliro wapaderadera wokufalitsa uthenga wabwino ku dziko lonse lapansi pakukhazikitsa timagulu ta anthu okhulupirira.

Mu m'manenedwe a lero lino amatchedwa mamishonare kapena odzala mipingo. Baibulo limakamba za magulu atumwi atatu osiyana. Yesu Khristu amatchedwa kuti mtumwi:

Potero, abale oyera mtima, olandirana nao maitanidwe akumwamba, lingirirani za Mtumwi ndi. Mkuluwansembe wa cibvomerezo cathu, Yesu ; amene anakhala wokhulupirika kwa iye adamuikayo, monganso Mose m'nyumba yace yonse. (Ahebri 3:1-2)

Ophunzira khumi ndi mmodzi aja amatchedwanso kuti atumwi:

Ndipo maina ao a atumwiwo khumi ndi awiri ndi awa: (Mateyu 10:2)

Atumwi khumi ndi awiri aja adali ndi ntchito yapaderadera. Anali mbali imodzi yodzala mpingo. Ngakhale kuti anali ndi ntchito imene okhulupirira ena sakanakhalanayo, palinso mphatso ya Mzimu Woyera ya utumwi:

Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi (Aefeso 4:11)

Malingana ndi ndime imeneyi, Mulungu ndi amene amasankha ena kukhala atumwi ndipo Paulo akuchitiranso umboni pa za izi:

Ndipotu Mulungu anailea ena m'Eklesia, poyamba arumwi. (1 Akorinto 12:28)

Baibulo limakamba za zizindikiro zapaderadera zotsimikiza kuti munthu ali ndi mphatso ya utumwi:

Zizindikilotu za ntumwi zinacitika pakati pa inu, ri'cipiriro conse, ndi zizindikilo, ndi cozizwa, ndi zamphamvu. (2 Akorinto 12:12)

Ndipo khamu lonse linatonthola; ndipo anamvera Bamaba ndi Paulo alikubwerezanso zizindikiro ndi zozizwitsa zimene Mulunguanacita nao pa amitundu.... (Macitidwe 15:12)

Utsogoleri wapaderadera wa atumwi pa mipingo wawonetseredwa mu buku la Machitidwe:

Ndipo anadza ena akutsika ku Yudeya, nawaphunzitsa abale, nati, Mukapandakudulidwa monga mwambo wa Mose, simungathe kupulumuka. Ndipo pamene Paulo ndi Bamaba anacitana nao makani ndi mafunsano, abale anapatula Paulo ndi Bamaba, ndi ena a iwo, kuti akwere kunka ku Yerusalemu kwa atumwi ndi akuru kukanena za funsolo. (Macitidwe 15:1-2)

Pamene anapita kupyola pamidzi, anapereka kwa iwo malamulo awasunge, amene analamulira atumwi ndi akuru a pa Yerusalemu. Kotero Mipingoyo inalimbikitsidwa m'cikhulupiriro, nacuruka m'ciwerengo cao tsiku ndi tsiku. (Macitidwe 16:4-5)

Atumwi amafalitsa uthenga Wabwino pakudzutsa mipingo. Amapereka utsogoleri ku mipingo imeneyi ndipo amakhala ndi zizindikiro zapaderadera mu utumiki wawo. Mayitanidwe ndi chikhumbo chokhala mtumwi chimachokera kwa Mulungu:

PAULO, mtumwi (wosacokera kwa anthu, kapena mwa munthu, koma mwa Yesu Kristu, ndi MulunguAtate, amene anamuukitsa iye kwa akufa), (Agalatiya 1:1)

Mphatso yapaderaderayi imazindikirika ndi mpingo umene umatumiza mtumwi ku malo ena:

Ndipo kunali aneneri ndi aphunzioo ku Antiokeya mu Mpingo wa komweko, ndiwo Barnaba, ndi Sumeoni, wonenedwa Nigeri, ndi Lukiya wa ku Kurene, Manayeni woleredwa pamodzi ndi Herode ciwangaco, ndi Saulo. Ndipo pa kutumikira Ambuye iwowa, ndi kusala cakudya, Mzimu Woyera anati, Mundipatulire Ine Bamaba ndi Saulo ku nchito imene odinawaitanirako. Pamenepo, m'mene adasala cakudya ndi kupemphera ndi kuika manja pa iwo, anawatumiza amuke... (Macitidwe 13:1-3)

Mtumwi amafunafuna kutumikira m'malo amene ena sanafikeko ndi uthenga wabwino:

ndipo coteri ndinaciyesa cinthu calemu kulalikira Uthenga Wabwino, pa malopo Kristu asanachullidwe kale, kuti ndisamange nyumba pa maziko a munthu wina. Koma monga kwalembedwa, Iwo amene uthenga wace sunawafikire, adzaona, Ndipo iwo amene sanamve, adzadziwitsa. (Aroma 15:20-21)

kukulalikira Uthenga Wabwino m'tsogolo mwace mwa inu, sikudzitamandira mwa cilekezere ca wina, ndi zinthu zokonzeka kale. (2 Akorinto 10:16)

Mtumwi amakhala okonzeka kukhala mu m'chikhalidwe cha anthu ena ndi cholinga chofuna kuwatengera anthuwo kwa Yesu Mkhristu:

Pakuti pokhala ndinali mfulu kwa onse, ndinadzilowetsa ndekha ukapolo kwa onse, kuti ndipindule ocuruka. Ndipo kwa Ayuda ndinakhala monga Myuda, kuti ndipindule Ayuda; kwa iwo omvera lamulo monga womvera lamulo, ngakhale sindinakhala ndekha womvera lamulo, kuti ndipindule iwo omvera malamulo; kwa iwo opanda lamulo monga wopanda lamulo, wosati wakukhala ine wopanda lamulo kwa Mulungu, koma womvera lamulo twa Kristu kuti ndipindule iwo opanda lamulo. Kwa ofoka ndinakhala ngati wofoka, kuti ndipindule ofoka, Ndakhala zonse kwa anthu onse, 1 kuti paliponse ndikapulumutse ena. Koma ndicita zonse zifukwa ca Uthenga Wabwino, kuti ndikakhale woyanjana nao. (1 Akorinto 9:19-23)

Mtumwi amadzutsa mipingo ndi utsogoleri ophunzitsidwa bwino umene utha kutipiriza ntchito yomwe mtumwi wayiyamba popanda iye:

Pamene analalikira Uthenga Wabwino pamudzipo, nayesa ambiri akuphunzira, anabwera ku Lustra ndi Ikoniyo ndi Antiokeya, nalimbikitsa mitima ya akuphunzira, nadandauliraiwo kuti akhalebe m'cikhulupiriro, ndi kuti tiyenera kulowa m'ufumu wa Mulungu zisautso zambiri. Ndipo pamene anawaikira akuru mosankha mu Mpingo Mpingo, ndi kupemphera pamodzi ndi kusala kudya, anaikiza iwo kwa Ambuye amene anamkhulupirirayo. (Macitidwe 14:21-23)

Vesi limeneli likuwulula kuti kuyendera mipingo ndi kudzutsa utsogoleri wodlalilika wa mipingo yatsopano ndi udindo wa mtumwi.

Chizindikiro ndi chitsimikizo cha mphatso ya utumwi ndi zotsatira zomwe zimawoneka m'miyoyo ya anthu ena. Paulo analemba mpingo wa ku Akolinto umene anawukhazikitsa:

Ngati sindiri mtumwi kwa ena, komatu ndiri kwa inu; pakuti cizindikilo ca utumwi wanga ndi inu mwa Ambuye. (1 Akorinto 9:2)

Kuthekera kodzutsa Madera a anthu okhulupirira komanso kuwapanga kuti akhale mpingo ndi chizindikiro cha mphatso ya utumwi.

Baibulo limachenjeza za utumwi abodza amene ndi onyenga koma atha kudziwika ndi ntchito zawo:

Pakuti otere ali utumwi onyenga, ocita ocenjerera, odzionetsa ngati utumwi a Kristu, Ndipo kulibe kudabwa; pakuti Satana yemwe adzionetsa ngati mngelo wa kuunika. Cifukwa cace sikuli kanthu kwakukuru ngatinso utumiki ace adzionetsa monga utumiki a cilungamo; amene cimariziro cao cidzakhala monga nchito zao. (2 Akorinto 11:13-15)

ZOWONJEZERA POPHUNZIRA:

Chipangano cha tsopano chimapereka zitsanzi zingapo za iwo amene adali ndi mphatso ya utumwi. Gwiritsani ntchito ma vesi ali m'musiwa kuti muphunzire zambiri:

-Paulo: Agalatiya 1:1

-Andironko ndi Yuniya: Aroma 16:7

-Apollo: I Akolinto 4:6,9

-Yakobo: Agalatiya 1:9

-Atumwi a Yesu: Mabuku a uthenga wabwino Wabwino wa Yesu ndi Machitidwe.

ANENERI

Ndipotu Mulungwanailea ena m'Eklesia, poyamba arumwi, aciwiri aneneri, acitatu aphunzitsi, pamenepo zozizwa, pomwepo mphatso zamaciritso, mathandizo, maweruziro, malilime a mitundu mitundu. (1 Akorinto 12:28)

Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; (Aefeso 4:11)

Pali mphatso za uneneri ziwiri. Yoyamba ndi mphatso yapaderadera ya kukhala mneneri. Ina ndi mphatso yoyankhula uneneri. Uneneri ndi kuyankhula pansi pakudzodzedwa ndi Mulungu. Ndikuthekera kolandira ndikupereka uthenga woyankhulidwa ndi Mulungu kupita kwa anthu ake kudzera mukuyankhula modzodzedwa. Mwa ichi, tanthauzo la uneneri ndi mphatso yapaderadera ya utsoholeri wa mneneri komanso mphatso yoyankhula uneneri.

Munthu samakhala mneneri chifukwa chakuti akunenera. Paulo adauza mpingo kuti afunefune mphatso yonenera:

Tsatani cikondi; koma funitsitsani mphatsozauzimu, koma koposa kuti mukanenere. (1 Akorinto 14:1)

Pakuti mukhoza nonse kunenera mmodzi mmodzi, kuti onse aphunzire, ndi onse afulumidwe; (1 Akorinto 14:31)

Koma Paulo anawonetsa kuti si aliyense amene ali mneneri. Iye anafunsa:

Kodi ali onse atumwi? Ali aneneri onse kodi? Ali aphunzitsi onse? Ali onse ocita zozizwa? (1 Akorinto 12:29)

Kusiyana pakati pa mneneri ndi kunenera kwawonetseredwa mu ndime zotsatirazi:

Ndipo m'mawa mwace tinacoka, ntinafika ku Kaisareya, ndipo m'mene tinalowa m'nyumba ya Filipo mlaliki, mmodzi wa asanu ndi awiri aja, tinakhala naye. Ndipo munthuyu anali nao ana akazi anai, anamwali, amene ananenera. Ndipo pokhalapo masiku ambiri, anatsika ku Yudeya mneneri, dzina lace Agabo. Ndipo anadza kwa ife natenga lamba la Paulo, nadzimanga yekha manja ndi mapazi, nati, Atero Mzimu Woyera, Munthu mwini lamba ili, adzammanga koteru Ayuda a m'Yerusalemu, nadzampereka m'manja a amitundu. (Macitidwe 21:8-11)

Ana akazi Filipo anali ndi mphatso yoyankhula ya uneneri. Koma Agabo adali mneneri amene samangopereka ma uthenga a uneneri koma adali ndi udindo wotsogolera mu mpingo. Mulungu amamugwiritsa ntchito iye mu udindo wotsogolera molingana ndi utumiki wa Paulo. Agabo

anapereka chitsogozo kwa Paulo zokhudza zimene zikamuchitikire Paulo ku Yerusalemu. (Machitidwe 21:11).

Amene ali ndi mphatso yapaderadera yakukhala ya mneneri samangoyankhula pansi pachitsogozo cha Mulungu. Iwo amakhala ndi udindo, ofesi ya ulamuliro ndi utsogoleri mu mpingo. Izi zikutsimikizidwa pa Machitidwe 13:1-4 pamene aneneri ndi aphunzitsi anagwiritsidwa ntchito mu utsogoleri kutsogolera Banaba ndi Saulo mu utumiki wapaderadera umene Mulungu anawayitanirako iwo.

Mu m'chipangano Chakale anthu amapita kwa aneneri kuti akapeze chitsogozo. Komaq nthawi imeneyi, mphatso yodzadzidwa ndi Mzimu Woyera inali isanaperekedwe. Kupezeka kwa Mulungu kumatsekedwa mmalo oyeretsetsa. Chifukwa cha imfa ndi kuwuka kwa Yesu Khristu, tsopano tili ndi kuthekera kwa kupezeka kwa Mulungu. Mphatso ya Mzimu Woyera yaperekedwa komanso monga mwaphunzira m'mbuyomu, chimodzi mwa zolinga zake ndikutsogolera:

Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu, (Aroma 8:14)

Panopa sizofunikanso kupita kwa mneneri kukafuna chitsogozo cha uzimu. Iyi ndi imodzi mwa ntchito za Mzimu Woyera mwa munthu okhulupirira. Okhulupirira aliyense akuyenera kuphunzira momwe angatsogoleredwe ndi mzimu wa Mulungu. Chipangano chatsopano sichikupereka chilichonse chokhudza anthu okhulupirira akukafuna chitsogozo kuchokera kwa aneneri kuchokera pomwe mphatso ya Mzimu Woyera inaperekedwa.

Koma Mulungu amagwiritsabe ntchito mphatsoyi kupereka chitsimikizo cha chitsogozo chomwe chilipo kale mwa okhulupirira kudzera mwa Mzimu Woyera. Izi ndi zimene zidachitika kwa Agabo ndi Paulo. Paulo anakadziwa kale kuti akuyenera kupita ku Yerusalemu. Uneneri wa Agabo unaulula zomwe zikamuchitikire kumeneko. Sunali uneneri wachitsogozo omuuza Paulo kuti apite kapena asapite ku Yerusalemu.

Mau amene amayankhulidwa ndi mneneri pansi potsogozedwa ndi kudzedwa ndi Mulungu amatchedwa kuti uneneri. Kunenera kumatanthauza kuti kukhazikitsa poyera mawu ochokera kwa Mulungu amene amalimbikitsa, kumangirira ndi kutonthonza:

Koma iye wakunenera alankhula ndi anthu comangirira ndi colimbikitsa, ndi cosangalatsa, (1 Akorinto 14:3)

Uneneri sumatumikira kwa anthu okhulupirira okha ayi kudzera mkumangirira komanso, koma umatumikiranso anthu osakhulupirira. Uneneri utha kutsutsa anthu osakhulupirira ndikuwapangitsa kuti abwere kwa Ambuye:

Koma ngati onse anenera, ndipo alowamo wina wosakhulupirira kapena wosaphunzira, atsutsidwa ndi onse; aweruzidwa ndi onse; zobisika za mtima wace zionetsedwa; ndipo coteru adzagwa nkhope yace pansi, nadzagwadira Mulungu, nadzalalikira kuti Mulunguali ndithu mwa inu. (1 Akorinto 14:24-25)

Chimodzi mwa zolinga za mneneri ndikubweretsa anthu kukulapa:

Koma Iye anawatumira aneneri kuwabwezeranso kwa Yehova, ndiwo anawacitira umboni; koma sanawamvera. (2 Mbiri 24:19)

Baibulo limanena kuti uneneri ndi mphatso yayikulu imene aliyense akuyenera kuyikhumba kuposa mphatso ya malilime:

Tsatani cikondi; koma funitsitsani mphatsozauzimu, koma koposa kuti mukanenere. Pakuti iye wakulankhula lilime salankhula ndi anthu, koma ndi Mulungu; pakuti palibemunthu akumva; koma mumzimu alankhula zinsinsi. Koma iye wakunenera alankhula ndi anthu comangirira ndi colimbikitsa, ndi cosangalatsa, (1 Akorinto 14:1-3)

Ndipo ndifuna inu nonse mula'nkhule malilime, koma makamaka kuti mukanenere; ndipo wakunenera aposa wakulankhula malilime, akapanda kumasulira, kuti Mpingo ukalandire comangirira. (1 Akorinto 14:5)

Cifukwa cace; abale anga, funitsitsani kunenera, ndipo musaletse kulankhula malilime. (1 Akorinto 14:39)

Mzimu Woyera nthawi zonse umateteza uneneri weniweni ndikutsogolera kukhazikika kwa anthu pa Yesu Mkhristu:

Koma za mphatso zauzimu, abale, sindifuna kuti mukhale osadziwa. Mudziwa kuti pamene munali amitundu, munatengedwa kunka kwa mafano aja osalankhula, monga munatsogozedwa. Cifukwa cace ndikuuzani inu, kuti palibe munthu wakulankhula mwa Mzimu wa Mulungu, anena, Yesu ngwotembereredwa; ndipo palibe wina akhoza kunena, Yew ali Ambuye, koma mwa Mzimu Woyera. (1 Akorinto 12:1-3)

Uneneri usatenge malo a mau a Mulungu olembedwa. Baibulo limati, uneneri udzatha koma mawu a Mulungu adzakhalapo mpaka kalekale:

Koma Mau a Mulunguakhala cikhali. Ndipo 10 mau olalikidwa kwa Inu ndi jawo. (... Petro 1:25)

Baibulo limachenjeza za aneneri onyenga (Mateyu 24:11,24; Marko 13:22). Munthu otchedwa kuti “mneneri wonyenga” adzazindikirika ndi zinthu zochitika mmasiku otsiriza a nthawi ya panso pano (Chivumbulutso 13:11-17; 16:13; 19:20; 20:10).

Chifukwa chakuti pali aneneri onyenga, mawu a Mulungu amapereka njira zingapo zozindikirira ma uneneri enieni. Mutha kuwazindikira:

1. KUPOTOZA CHIPHUNZITSO CHA BAIBULO:

Ndipo pokhala ife ndi mphatso zosiyana, monga mwa cisomo copatsidwa kwa ife, kapena mphatso yakunenera, tinenere monga mwa muyeso wa cikhulupiriro; (Aroma 12:6)

Mawu akuti “mwa mulingo wa chikhulupiriro” akutanthauza kuti mwa ubale wabwino ndi chikhulupiriro. Njira yozindikirira ma uneneri enieni ndikuwona ngati uneneriwo ukugwirizana ndi chiphunzitsa cha chikhristu chimene chivumbulutsidwa m’Baibulo. Mwachitsanzo, aneneri onyenga samavomereza u Mulungu wa Yesu Mkhristu:

Okondedwa, musamakhulupirira mzimu uli wonse, koma yesani mizimu ngati icokera mwa Mulungu: popeza aneneri onyenga ambiri anaturuka kulowa m'dziko lapansi. M'menemo muzindikira Mzimu WI Mulungu: mzimu uli wonse umen ubvomereza kuti Yesu Kristu ana dza m'thupi, ucokera mwa. Mulungu (1 Yohane 4:1-2)

Aneneri onyenga amaphunzitsa za chiwerewere ndi kuledzerela:

Koma padakhalanso pakati pa anthuwo aneneri onama, monganso padzakhala aphunzitsi onama pakati pa inu, amene adzalowa nayo m'tseri mipatuko yotayikitsa, nadzakana Ambuye amene adawagula, nadzadzitengera iwo okha citayiko cakudza msanga. Ndipo ambiri adzatsata zonyansa zao; cifukwa ca iwo njira ya coonadi idzanenedwa zamwano. Ndipo m'cisiriro adzakuyesani malonda ndi mau onyenga; amene ciweruzo cao sicinacedwa ndi kale lomwe, ndipo citayiko cao siciodzera. 2 Petro 2:1-3

Aneneri onyenga amayesa kuwakokera kutali, kuwachotsa kukumvera mawu a Mulungu. (Deteronomo 13:1-5).

Uneneri ngati umenewu suli pa mulingo wabwino wa chikhulupiriro cha chikhristu.

2. ZIZINDIKIRO ZA ANENERI ONYENGA:

Aneneri onyenga amawanamiza anthu ndi zizindikiro zozwizwa:

Ndipo aneneri onama ambiri adzauka, nadzasokeretsaanthuambiri. cifukwa Akristu onama adzauka, ndi aneneri onama nadzaonetsa zizindikiro zazikuru ndi zozizwa: kotero kuti akanyenge, ngati nkotheke, osankhidwa omwe. Onani ndakuuziranitu pasadafike. (Mateyu 24:11,24)

3. CHIPATSO CHOIPA:

Chizindikiro cha chipatso cha mzimu ndi muyeso weniweni wa utumiki uliwonse:

Yang'anirani mupewe aneneri onyenga, amene adza kwa inu ndi zobvala zankhosa, koma m'kati mwao ali afisi alusa. Mudzawazindikira ndi zipatso zao. Kodi achera mphesa paminga, kapena nkhuju pamtula? (Mateyu 7:15-16)

Mu m'chaputala 11 muphunzira za chipatso cha Mzimu Woyera. Zimenezi ndi zizindikiro za uzimu zimene mmneneri onyenga amakhala nazo.

4. KUDZIKUZA:

Mneneri aliyense amene amanena kuti ndi wofanana ndi khristu ndi wonyenga:

Pomwepo munthu akanena kwa inu, Onani, Kristu ali kuno, kapena uko musambvomereze; cifukwa Akristu onama adzauka, ndi aneneri onama nadzaonetsa zizindikiro zazikuru ndi zozizwa: kotero kuti akanyenge, ngati nkotheka, osankhidwa omwe. Onani ndakuuziranitu pasadafike. (Mateyu 24:23-24)

5. MAUNENERI OSAKWANIRITSIDWA:

Muyeso womaliza umene mneneri wabodza tingamudziwire ndikuwona ngati zimene akunenera zikukwaniritsidwa kapena ayi:

Koma mneneri wakucita modzikuza ndi kunena mau m'dzina langa, amene sindinamlamulira anene, kapena kunena m'dzina la milungu yina, mneneri ameneyo afe. Ndipo mukati m'mtima mwanu, Tidzazindikira bwanji mau amene Yehova sananena? Mneneri akanena m'dzina la Yehova, koma mau adanenawa sacitika, nisafika, ndiwo mau Yehova sanawanena; mneneriyo ananena modzikuza, musamuopa iye. (Deuteronomo 18:20-22)

ZOWONJEZERA POPHUNZIRA:

Uneneri utha kuchokera patatu:

-Mzimu wa munthu: Yeremia 23:16; Ezeieli 13:2,3

-Mizimu woyipa ndi yabodza: Yesaya 8:19-20; IMfumu 22:22; Mateyu 8:29;

Machitidwe 16:17

-Mzimu Woyera: II Samueli 23:2; Yeremia 1:9; Machitidwe 19:6; 21:11

Ichi ndichifukwa chake tiziyesa ma uneneri kuti tidziwe ngati akuchokera kwa Mzimu Woyera.

Baibulo limapereka zitsanzo zambiri za aneneri a m'chipangano chakale kuti muphunzire ndikukulitsa chidziwitso chanu cha aneneri ndi mphatso ya uneneri. Pamene mukuwerenga ndimezi yesani kusiyantsa iwo amene anali ndi mphatso ya kukhala mneneri [utsogoleri] ndi iwo amene anali ndi mphatso yakunenera chabe.

Aneneri achipangano Chakale

Abrahamu:	Genesis 20:7
Mose:	Deuteronome 34:9
Habakuku:	Habakkuk 1:1
Yesaya:	II Mafumu 19:2
Mika:	Mateyu 2:5-6
Hoseya	Mateyu 21:15
Eferemu:	Hoseya 9:8
Yoweri:	Machitidwe 2:16
Jeremiya:	Yeremiya 1:5
Gadi:	I Samuel 22:15

Zakariya:	Zakariya: 1:1
Ahijah:	I Mafumu 11:29
Samueli:	I Samuel 3:20
Jehu:	I Mafumu 16:7
Natani:	II Samuel 7:2
Mikaya:	II Mbiri 22:7-8
Jona:	II Mbiri 14:25
Iddo:	II Mbiri 13:22
Azzu:	Yeremiya 28:1
Ezekieli:	Ezekieli 2:1-5
Hananiya:	Yeremiya 28:17
Danieli:	Mateyu 24:15
Balaam:	II Petro 2:15-16
Amosi:	Machitidwe 7:42-43
Shemi:	II Mbiri 12:5
Elisa:	I Mafumu 19:16
Eliya:	I Mafumu 18:22
Haggai:	Haggai 1:1
Davide:	Machitidwe 2:29-30
Aroni:	Eksodo 7:1
Azariya:	II Mbiri 15:8
Obedi:	II Mbiri 15:8
Asafu:	Salimo 78:2

Aneneri mu Chipanga Chakale (Azimayi):

Miriyamu:	Eksodo 15:20
Debora:	Oweruza 4:4
Hulda:	II Mafumu 22:14
Noadia:	Nehemiya 6:14
Mkazi wa Yesaya:	Yesaya 8:3

Aneneri a Chipangano chatsopano:

Yesu:	Mateyu 21:11
Yohane M'batizi:	Mateyu 11:7-11
Agabasi:	Machitidwe 11:27-28; 21:10
Judasi:	Machitidwe 15:32
Sila:	Machitidwe 15:32
Atsogoleri aku Antiyokeya:	Machitidwe 13:1

Aneneri a chizimayi mu chipangano chatsopano:

Anna:	Luka 2:36
Ana akazi a Filipi:	Machitidwe 21:8-9

Werengani ndondomeko zogwiritsira ntchito uneneri pamene mpingo wakumana pa 1 Akorinto 14:29-31.

ALARIKI

Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; (Aefeso 4:11)

Mlariki ali ndi kuthekera kogawana ndi anthu ena Uthenga Wabwino munjira imene anthu ena osankhulupirika amakopeka nako ndi kukhala mbali imodzi ya thupi la Yesu Khristu. Tanthauzo la mlariki ndi munthu amene amafaritsa uthenga Wabwino.

Mau oti mlariki amapezeka katatu kokha mu Chipangano Chatsopano. Mu buku la Aefeso amatchulidwa ngati mphatso imodzi ya Mzimu Woyera:

Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi ena aneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; (Aefeso 4:11)

Ngakhale kuti anthu onse amene ndi okhulupirira ayenera kulalika uthenga Wabwino, koma pali anthu ena amene anachita kupatsidwa mphatso yolalika uthenga Wabwino. Pamene Filipino anakumana ndi Natanieli, chinthu choyamba chinali kugawana naye Uthenga Wabwino.

Ndipo m'mawa mwace tinacoka, ntinafika ku Kaisareya, ndipo m'mene tinalowa m'nyumba ya Filipino mlaliki, mmodzi wa asanu ndi awiri aja, tinakhala naye. (Machitidwe 21:8)

Filipo ndi munthu yekhayo amene akutchedwa ngati mlariki mu Chipangano chonse Chatsopano. Zoti iye ndi mlariki zinaonekeratu pachiyambi pamene anakumana ndi Yesu. Iye atakumana ndi Yesu, chinthu choyamba chimene anachita kunali kugawana ndi Natanieli uthenga Wabwino.

Filipo anapeza Natanayeli, nanena naye, iye 12 amene Mose analembera za iye m'cilamulo, ndi aneneri, tampeza, ndiye Yesu mwana wa Yosefe wa ku Nazarete. Natanayeli anati kwa iye, 13 Ku Nazarete nkutha kucokera kanthu kabwino kodi? Filipino ananena naye, Tiye ukaone. (Yohane 1:45-46)

Patapita kanthawi, Filipino anatsogolera kulalikira Uthenga wabwino kwa Aheleni:

Ndipo iwo anadza kwa Filipino wa ku Betsaida wa m'Galileya, namfunsa iye, ndi kuti, Mbuye, tifuna kuona Yesu. (Yohane 12:21)

Filipo anasankhidwa ngati ophunzira wa Yesu Khristu (Mateyu 10:3) ndipo Iye anali nawo muchipinda cha pamwamba pamene Mzimu Woyera unatsika (Machitidwe 1:13) Iye anadzodzedwa ngati mdindo wa mu mpingo (Machitidwe 6:1-6) ndipo iye anakhazikitsidwa ndi Mulungu ngati mlariki (Aefeso 4:11-12)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Pitirizani kuphunzira za utumiki wa Filipino kuti mukuze chidziwitso chanu cha mphatso ya mlariki:

-Uthenga wake:

Machitidwe 8:35

-Mamasuridwe, Zozizwitsa, Machritso:

Machitidwe 8:5-8

- Kubatizidzwa: Machitidwe 8:12,36-38
 - akulalikira Uthenga Wabwino]: Machitidw 8:12
 - Kukhazikitsa dongoro: Machitidwe 21:8-9
 - Ayenda Maulendo kufalitsa Uthenga Wabwino: Machitidwe 8:4-5,26,40
 - Kuthekera kokopa anthu: Machitidwe 8:6
 - Anagwedeza Mizinda: Machitidwe 8:8
 - Anatumikira kwa anthu: Machitidwe 8:27-38
 - Kutsogozedwa ndi Mulungu: Machitidwe 8:26,39
 - Chidziwitso cha Mau a Mulungu: Machitidwe 8:30-35
- Amadziwika chifukwa chakuchita bwino pa Utumiki komanso kutembenuka mtima kwa anthu (Machitidwe Machitidwe 8:5-6,8,12,35-39)

ABUSA

Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; (Aefeso 4:11)

Malingana ndi Baibulo la chi Heleni, mau oti m'busa amatanthauza munthu oweta ziweto monga m'busa wa nkhosa. Azibusa ndi anthu amene amatenga udindo oyang'anira umoyo wauzimu wa anthu ena. Chifukwa cha tanthauzo la mau amenewa, munthu amene akudzitcha kuti ndi m'busa ayenera kutsata chitsanzo chabwino cha Yesu amene ndi m'busa wa anthu.

Koma Mulunguwa mtendere amene anabwera naye woturuka mwa akufa 1 Mbusa wamkuru wa nkhosa 2 ndi mwazi wa cipangano cosatha, ndiye Ambuye wathu Yesu, (Ahebri 13:20)

Ndipo pakuonekera Mbusa wamkulu, mudzalandira korona wa ulemerero, wosafota. Momwemonso, anyamata inu, mverani akulu. (1 Petro 5:4)

zinthu zoyenera munthu kuti akhale mkulu wampingo, mdindo, mlariki ndi zomwezonso zimene m'busa ayenera kukwaniritsa. Werengani I Timoteo 3:1-13.

Udindo wauzimu wa m'busa ndi oti adyetse komanso kuteteza anthu amene amuzungulira. Koma izi zikuyenera kuchitika ndi cholinga choyenera osati ndalama chabe:

Tadzicenjerani nokha, ndi gulu lonse, pamenepo Mzimu Woyera anakuikani oyang'anira, kuti muwete Eklesia wa Mulungu, umene anaugula ndi mwazi wa iye yekha. (Macitidwe 20:28)

Wetani gulu la Mulunguliri mwa inu, ndi kuliyang'anira, osati mokangamiza, koma mwaufulu, kwa Mulungu; osatsata phindu lonyansa, koma mwacangu; osati monga ocita ufumu pa iwo a udindo wanu, koma okhala zitsanzo za gululo. Ndipo pakuonekera Mbusa wamkulu, mudzalandira korona wa ulemerero, wosafota. Momwemonso, anyamata inu, mverani akulu. (1 Petro 5:2-4)

Mau oti m'busa mu Chipangano Chakale amapezeka mu buku la Yerememiya lokha. Pa ndimene imeneyi, Mulungu akuchenjeza abusa:

Yeremiya 2:8 ndi abusa omwe anandilakwira Ine, (Yeremiya2:8)

Pakuti abusa apulukira, sanafunsire kwa Yehova; cifukwa cace sanapindula; zoweta zao zonse zabalalika. (Yeremiya 10:21)

Abusa ambiri aononga munda wanga wamphesa, apondereza gawo langa, pondikondweretsa apayesa cipululu copanda kanthu. Apayesa bwinja; pandilirira ine, pokhala bwinja; dziko lonse lasanduka bwinja; cifukwa palibe munthu wosamalira. (Yeremiya 12:10-11)

Tsoka abusa amene athetsa nabalalitsa nkhusa za busa langa! ati Yehova. Cifukwa cace atero Yehova, Mulunguwa Israyeli, ponenera abusa amene adyetsa anthu anga: Mwabalalitsa zoweta zanga, ndi kuzipitikitsa, ndipo simunazizonda; taonani, ndidzakusenzani inu kuipa kwa nchito zanu, ati Yehova. (Yeremiya 23:1-2)

POPITIRIZA KUPHUNZIRA:

Werengani zinthu zomuyenereza munthu kukhala ndi udindo mu mpingopa 1 Timoteo 3:1-13. Ndi zoyenereza zimenezi zimagwiranso ntchito kwa amene akufuna kutumukira ngati abusa. Werengani zokhudza makhalidwe a m'busa Wabwino malinga ndi Yohane 10:1-18.

APHUNZITSI:

Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; (Aefeso 4:11)

Mphunzitsi ndi munthu amene akhala ndi kuthelera kofotokozera mau a Mulungu mu njira imene anthu amatha kugwiritsa ntchito mfundo zimene zikuphunzitsidwazo. Kuphunzitsa sikungowana ndi anthu zimene Baibulo limaphunzitsa koma ndi kuphunzitsa anthu kuti achite zimene zikuphunzitsidwazo.

Kuti tisakhalenso makanda, ogwedezekagwedezeka, natengeka-tengeka ndi mphepo yonse ya ciphunzitso, ndi tsenga la anthu, ndi kucenjerera kukatsata cinyengo ca kusoceretsa; And He gave some...teachers... (Aefeso 4:14)

Ndipotu Mulungu Anaika ena m'Eklesia, p, acitatu aphunzitsi, (1 Akorinto 12:28) kapenayakutumikira, tidzipereke ku utumiki uwu; kapena iye wakuphunzitsa, kukuphunzitsako; (Aroma 12:7)

Siwina aliyense amene anakhale ndi mphatso ya uphunzitsi:

Ali aphunzitsi onse? (1 Akorinto 12:29)

Yankho la fuso ili ndi lakuti “ayi” siwina aliyense amene a amalandira mphatso yauphunzitsi.

Mphatso yapadera yauphunzitsi imasiyana ndi mphatso yodziwa kulankhula. Ngati mukukumbukira, malingana ndi Machitidwe 13:1-4 zikuoneka kuti aphunzitsi ali ndi udindo wapadera mumpingo chimodzimidzi ndi aneneri. Siokhulupilira wina aliyense amene ali ndi

mphatso yauphunzitsi koma ngakhale izi ziri chonchi, okhulupirira wina aliyense ali ndi udindo ofotokozera mfundo zofunika kwambiri za uthenga Wabwino:

Pakuti mungakhale mwayenera kukhala aphunzitsi cifukwa ca nyengoyi, muli nako kusowanso kuti wina aphunzitse inu zoyamba za ciyambidwe ca maneno a Mulungu; ndipo mukhala onga ofuna mkaka, osati cakudya cotafuna. (Ahebri 5:12)

Okhulupirira wina aliyense amene ndi okhwima ayenera kutenga gawo pakuphunzitsa uthenga Wabwino posatengelera kuti ali ndi mphatso yauphunzitsi kapena ayi. (chifukwa cha ichi, Harvestime International Institute ili ndi phunziro lapadera lotchedwa. “*Ukadaulo ophunzitsa*” ndi cholinga chopereka chidziwitso chambiri.

Baibulo limachenjeza za aphunzitsi onyenga. Awa ndi anthu amene amati ali ndi mphatso yauphunzitsi koma samaphunzitsa mau a Mulungu owonadi:

Koma padakhalanso pakati pa anthuwo aneneri onama, monganso padzakhala aphunzitsi onama pakati pa inu, amene adzalowa nayo m'tseri mipatuko yotayikitsa, nadzakana Ambuye amene adawagula, nadzadzitengera iwo okha citayiko cakudza msanga. Ndipo ambiri adzatsata zonyansa zao; cifukwa ca iwo njira ya coonadi idzanenedwa zamwano. (2 Petro 2:1-2)

Pakuti idzafika nthawi imene sadzalola ciphunzitso colamitsa; komatu poyabwa m'khutu adzadziuniikitsa aphunzitsi monga mwa zilakolako za iwo okha: ndipo adzalubza dala pacoonadi, nadzapatukira kutsata nthanu zacabe. (2 Timoteo 4:3-4)

**Atate wako woyamba anacimwa, ndi otanthauzira ako andilakwira Ine....
(Yesaya 43:27)**

Pa II Petro 2 ndi Yuda, akufotokoza makhalidwe amene amaonetsera ngati munthu ndi mphunzitsi woonadi kapena ayi:

Munthu akhoza kukhala ndi zolinga zolakwika pophunzitsa.

amene ayenera kutsekedwa pakamwa; ndiwo amene apasula mabanja banja lonse, ndi kuphunzitsa zosayenera cifukwa ca cisiriro conyansa. (Tito 1:11)

Anthu amene amaphunzitsa mau a Mulungu ayenera kuphunzitsa okholupirira amene akhonza kuphunzitsa anthu ena.

Koma iye amene aphunzira mau, ayenera kucereza womphunzitsayo m'zonse zabwino. (Agalatiya 6:6)

lalikira mau; cita nao pa nthawi yace, popanda nthawi yace; tsutsa, dzudzula, cenjeza, ndi kuleza mtima konse ndi ciphunzitso. (2 Timoteo 4:2)

Ichi ndi chifaniziro chabwino chimene chiyenera kutsatidwa ndi cholinga chofuna kuchulukitsa aphunzitsi ofalitsa mau a Mulungu.

Munthu amene ali ndi mphatso ya uphunzitsi samaphunzitsa mzeru ya munthu:

Zimenenso tilankhula, si ndi mau ophunzitsidwa ndi nzeru za munthu, koma ophunzitsidwa ndi Mzimu; ndi kulinganiza zamzimu ndi zamzimu. (1 Akorinto 2:13)

Mphunzitsi ayenera kukhala ndi mzeru ya Mulungu. Paulo akuchenjeza iwo amene...

pofuna kukhala aphunzitsi a lamulo ngakhale sadziwitsa zimene azmena, kapena azilimbikirazi. (1 Timoteo 1:7)

Iye akutsindika kufunika kophunzitsa ndi mzeru:

kwa iwo amene Mulunguanafuna kuwazindikiritsa ici 6 cimene ciri cuma ca ulemerero wa cinsinsi pakati pa amitundu, ndiye Kristu mwa inu, ciyembekezo ca ulemerero; amene timlalikira ife, ndi kucenjeza munthu ali yense 7 ndi kuphunzitsa munthu ali yense mu nzeru zonse, 8 kuti tionetsere munthu ali yense wamphumphu mwa Kristu; (Akolose 1:27-28)

Mphunzitsi ayenera kukhala chimene iye amaphunzitsa:

ndiwe tsono wakuphunzitsa wina; kodi ulibe kudziphunzitsa mwini? iwe wakulalikira kuti munthu asabe, kodi ulikuba mwini wekha? Iwe wakunena kuti munthu asacite cigololo, kodi umacita cigololo mwini wekha? Iwe wakudana nao mafano, umafunkha za m'kacisi kodi? (Aroma 2:21-22)

Mphunzitsi adzawerizidwa malinga ndi zimene amaphunzitsa:

Musakhale aphunzitsi ambiri, abale anga, podziwa kuti tidzalangika koposa. (Yakobo 3:1)

POPITIRIZA KUPHUNZIRA:

Werengani zitsanzo za aphunzitsi mu Chipangano Chatsopano. Kodi ndi ndani amene mukuona kuti anali ndi mphatso yapadera ya uphunzitsi? Ndipo ndi ndani amene nali ndi mphatso yolankula yakuphunzitsa?

-Apolo:	Machitidwe 18:24-25
-Priska:	Machitidwe 18:26
-Paulo:	Machitidwe 20:20-21,27; 21:28
-Munthu osatchulidwa:	Machitidwe 13:1
-Petro:	Machitidwe 5:28-29

Pezani phunziro lina la Harvestime International Institute lotchedwa” *ukadaulo wakaphunzitsidwe*”

UTSOGOLERI KUGWILIRA NTCHITO LIMODZI

Mphatso zisanu zautsogoleri zimagwira ntchito limodzi pa utumiki wa mpingo.

Atumwi amafaritsa Uthenga Wabwino kumadera osiyanasiyana. Mulungu amapereka zizindikiro za zozizwizitsa ndi zodabwitsa kuti izi zithandize kufalitsa uthenga Wabwino. Atumwi amapereka utsogoleri wapadera mu mpingo ndipo amathandiza kukuza mipingo.

Aneneri: Amapereka utsogoleri mu mpingo ndi udindo wao mu mping kupereka uthenga ochokera kwa Mulungu mothandizidwa ndi Mzimu Woyera.

Alaliki amafaritsa Uthenga Wabwino munjira yoti anthu amaulandira uthengao ndikukhala okhulupilira. Iwo amatha kutumikira ku gulu ala anthu ochepa kapena ambira, koma iwo utumiki wao umabala zipatso za okhulupirira atsopano. Okhulupirira amene abadwa mwatsopano amakhala pansu pa m'busa, mneneri kapena aphuzitsi amene ali mu mpingo. Chitsanzo chabwino ndi Filipino amene atalalikira uthenga Wabwino kwa a Samariya, anawasiya mmanja mwa atumwi ndi cholinga choti aphunzitsidwe bwino.

Azibusu: Ali ndi udindo otsogolera anthu amena atembunenuka mtima kudzera mu utumiki wa alaliki. Iwo amapereka chisamaliro kwa nkhusa zao. Uwo utumiki wao uli ngati ubusa wankhusa

Aphunzitsi: iwo amapereka chiphunzitsa chozama chimene chimopyola mlingo umene mlaliki amapereka. Amaphunzitsa ophunzira kuti akule moyo wao wauzimu. Amaphunzitsa okhulupirira kuti akathe kuphunzitsa anthu ena.

Udindo weniweni wa anthu emene ali ndi udindo wautsogoleri ndi kuphunzitsa anthu ena kuti akazindikire mpatso yao yauzimu (Aefeso 4:11-16. Chithunzi chili pansichi chikuonetsa mmene mpatso zimagwilira ntchito limodzi mu mpingo.

MULUNGU




AMAPEREKA

ATUMWI ANENERI ALARIKI ABUSA APHUNZITSI



NDI CHOLINGA CHOKONZEKERETSA OKHULUPIRIRA
AMANE AKHOZA



KUTUMIKIRA KUPINDURITSA



NDIKUPANGITSA KUTI

PAKHALE UMODZI CHIDZIWITSO UNGWIRO



NDI CHOLINGA CHOTI THUPI LA KHRISTU LIKHALE



LOPANDA ANA

IYE

LUKULE MWA

(chiphunzitso chonyenga)

(Choonadi)



ZOTSATIRA ZAKE ZOMALIZA NDI IZI:
MAGAWO ONSE A THUPI LA KHRISTU AMAYENDA BWINO

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

2. Tchulani mpatso zisanu zautsogoleri zimene zakambidwa mu chaputala ichi

3. Ndi chifukwa chiani izi zimatchedwa mpatso zapadera?

4. Werangani ziganizo zili munsimuzi ndipo ngati chiganizochi chili cholondora lembani T pa mpata waperekedwao. Ndipo ngati chiganizochi chili chosalondora, lembani F.

- _____ wina aliyense amene amalosera amakhala kuti ali ndi mpatso yapadera yokhala mneneri
- _____ si wina aliyense amene amaphunzitsa amene ali ndi mpatso yauphunzitsi.
- _____ okhulupirira wina aliyese akuyenera kuphunzitsa uthenga Wabwino koma izi sizikutanthauza kuti wina aliyense ndi mphunzitsi.

5. Werangani mpatso imene yalembedwa mu mndandanda oyamba ndipo kenako werangani chiganizo chimene chalembedwa mu mndandanda wachiwiri. Kenako lembani nambala imene ikufotokozera tanthauzo la mpatso.

Mndanda oyamba

mdanda wachiwiri

2. _____ Mneneri

1. Amatumizidwa ndi ulamuliro oti akhazikitse mipingo ndikuyinga'anira

_____ Mtumwi

2. Amalankhula motsogozedwa ndi Mulungukuti apereka uthenga wake kwa anthu Ake a Mulungukomanso amakhala ndi udindo wautsogoleri

_____ M'busa

3. Amafaritsa Uthenga Wabwino kwa anthu osakhulupirira munjira yoti anthu Anthu amatembenuka mtima ndi kukhala gawo limodzi la mpingo

_____ Mlariki

4. Amatenga udindo wautsogoleri mu mpingo osamalira nkhoa kapena kuti zosowa Zauzimu za anthu mu mpingo.

_____ mpunzitsi

5. Amapereka uthenga wa mau a Mulungumunjira imene anthu amatha kuphunzira Komanso ndi kutha kuzigwiritsa ntchito zinthuzo.

6. Tchulani magawo anayi a akulu amene agwiritsidwa ntchito pofuna kusanthula mpatso zauzimu.

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa Buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Zoonjezera pophunzira zaperekedwa mu gawo lina lila lirilonse la chaputala ichi. Cholinga cha izi ndi chakuti zikuthandizeni kuti mumarize maphunziro anu musanapite gawo lina. Okhulupilira amene ali ndi mphatso zapadera mu mpingo amakhala atsogoleri.

Ma udindo a mkulu wa mpingo amatchuridwa mu Chipangano Chatsopano. Udindo wau Bishopu umachulidwa. Anthu ena amaganiza kuti udindo wa Bishopi ndi chimodzimodzi ndi udindo wa ubusa. Mpingo oyamba unaonetsera chitsanzo cha zinthu mmene zikuyenera kukhalira mu mpingo. Gwiritsani ntchito mndanda uli munsiu kuti muphunzire zambiri za maudindo atsogoleri mu mpingo.

ADINDO MU MPINGO

Udindo	ndime	ntchito yawo
Woyang'anira	I Timoteo 3:1-7 Afilipo 1:1 Tito 1:5-9 I Petro 5:2-3	Ambira amati udindo uwu ndi chimodzimodzi ndi udindo wa ubusa koma ma vesi awa sakuonetsera kuti iye anali ndi Ndi udindo osamala nkhosha kwa nthawi yaitali
Atumiki	I Timoteo 3:8-13 Afilipo 1:1 Machitidwe 6:1-7	Ma vesi awa akuonetsera kuti atumiki ali ndi udindo Otumikira ndi othandizira
Akazi	I Timoteo 3:11 Aroma 16:1-2	Akazi sakutchulidwa malingana ndi Baibulo. Matchalitchi ena Amati awa ndi akazi a atumiki kapena kuti awa ndi azimayi amene amtumikira Ndikuthandizira
Akulu	Machitidwe 20:17,28-32 Machitidwe 14:23;15 I Timoteo 5:17 I Petro 5:1-4 Tito 1:5; Yakobo 5:14	Ma vesi awa amaonetsera kuti akulu amapereka utsogoleri mu mpingi komanso ndi kupanga ziganizo. Iwonso amatumikira kuzosowa za mu mpingo ndi kuthandizira zinthu mu chitukuko cha mpingo

Mau oti akulu anagwiritsidwa ntchito koyambilira mu Buku la Eksodo 3:16. Pa ndime imeneyi akutchula atsogoleri a Israeli. Koma mau oti akulu a Israelio amatchulidwa malo ambiri mu Baibulo. Koma akulu ndi osiyana ndi akulu a mumpingo oyamba wa atumwi. Mavesi onse amene tapereka akutanthauza za akulu a mumpingo osati akulu a Israeli.

Ntchito ya atsogoleri ndi kupereka utsogoleri pamodzi ndi atsogoleri ena mumpingo amene Mulungu anakhazikitsa. Mulungu anakhazikitsa atsogoleri mu mpingo koma mpingo umasankha akulu.

ZOYENEREZA ATSOGOLERI

(I Timoteyo 3:2; Tito 1:6,7, Tito1:8; I Timoteo3:2, Tito 1:8)

- Akhale opanda chilema kapena banga (ayenera kukhala ndi mbiri yabwino komanso oyenda malingana ndi mau a Mulungu)
- Ayenera kukhala mamuna odziretsa
- Odziletsa mumagawo onse amoyo wake
- Osaledzera
- Odziwa kuchereza alendo (Khomu lake liyenera kukhala lotseguka kwa onse)
- Otha kuphunzitsa (okhala ndi kuthekera kolankula mau a Mulungu)
- Osamwetsa vinyo
- Osapya mtima msanga
- Asakhale obadwa kumene mwatsopano.
- Akonda chabwino
- Wangwiro
- Woyera
- Okhala ndi mbiri yabwino pakati pa anthu akunja

Akulu

- Ayenera kukhala odzilemekeza
- Asakhale okamba pawiripawiri.
- Otha kuweruza ana ake
- Otha kuyang'anira banja lake.
- Osakhale okonda ndalama.

DONGOSOLO LA MPINGO
Mpatso zautsogoleri zapadera

I

Atumwi

I

Aneneri

I

Alaliki

I

Abusa

I

Aphuzitsi

I

(aefeso 2-20-22)

I

(mothandizidwa ndi ma udindo a akulu, oyang'anira ndi anthu ena onse a mumpingo amene
amgwiritsa ntchito mpatso zao mu mpingo zimene Mulungu anakhazikitsa)

I

Maziko okhazikitsidwa ndi atumwi ndi aneneri

Mateyu 16:18, I Akorinto 3:11, Aefeso 2:20

CHAPUTALA 7

MPHATSO ZOLANKHULA ZA MZIMU WOYERA.

ZOLINGA

Pamapeto pa chaputala ichi, muyenera kudziwa zinthu izi:

- Kuzindikira mphatso zisanu zokhudza kulankhula.
- Kufotokoza tanthauzo la mphatso zolankhula.
- Kusiyanitsa pakati pa mau a Mzeru ndi mau a chidziwitso.

VESI YOTSOGOLERA:

**Koma tsopano, Mulungwanaika ziwalo zonsezo m'thupi, monga anafuna.
(1 Akorinto 12:18)**

MAU OYAMBA

Pali mphatso zisanu zimene zimatchedwa mphatso zolankhula chifukwa chakuti mphatsozi zimalira kuti munthu alankule. Ndipo mphatso zimenezi ndi izi:

- Uneneri
- Kuphunzitsa
- Kudandaulira
- Mau a mzeru
- Mau a chidziwitso.

Mphatso ya uneneri ndi yauphunzitsi zimafanana. Koma mphatso yolankhula ya uneneri ndi yophunzitsa zimasiyana ndi mphatso yautsogoleri okhala mneneri kapena mphunzitsi.

**ndi kwa wina macitidwe a mphanvu; ndi kwa wina cinenero; ndi kwa wina
cizindikiro ca mizimu; kwa wina malilime a mitundu mitundu; ndi kwa wina
mamasulidwe a malilime. (Akorinto 12:10)**

Munthu amene ali ndi mphatso yauneneri amalankhula zinthu zimene Mulungu wamuuza kupita kwa anthu. Mphatso ya uneneri inakambidwa mwatsatanetsane mu gawo limene timaona za mphatso yokhala mneneri. Mphatso yolankhula ya uneneri simaonetsera kuti munthu ali ndi mphatso yokhala mneneri. Koma ngati mmene tinaonera Mulungu anakhazikitsa anthu mu utsogoleri wa mpingo amene ali ndi mphatso yapadera ya uneneri.

Ngakhale kuti anthu ena amanenera ngati aneneri, anthu amene ali ndi mphatso ya uneneneri alibe mphatso udindo wapadera wauneneri. Iwo ntchito yawo ntchito yawo ndi kungopereka uthenga umene mothandizidwa ndi Mzimu Woyera apatsidwa.

KUPHUNZITSA

Ndipo pokhala ife ndi mphatso zosiyana, monga mwa cisomo copatsidwa kwa ife, kapena mphatso yakunenera, tinenere monga mwa muyeso wa cikhulupiriro; kapenayakutumikira, tidzipereke ku utumiki uwu; kapena iye wakuphunzitsa, kukuphunzitsako; (Aroma 12:6-7)

Mutu okhudza chiphunzitso unakambidwa kale pamene timaona zokhudza mphatso yapadera yauphunzitsi. Chifukwa cha ichi, zimene tinakambirani sizikusiyana ndi zimene zikambidwe apa.

Chimodzimodzi ndi mmene tinakambira ndi mpatso yauneneri, kukhala ndi kuthekera kophunzitsa sizimatanthauza kuti munthu ali ndi mphatso yapadera yophunzitsa. Mulungu anakhazikitsa anthu ake mu mpingo amene ali ndi mphatso yophunzitsa komanso udindo wapadera mumpingo.

KUDANDAULIRA

Ndipo pokhala ife ndi mphatso zosiyana, monga mwa cisomo copatsidwa kwa ife, kapena mphatso yakunenera, tinenere monga mwa muyeso wa cikhulupiriro; kapena iye wakudandaulira, kukudandaulirako; wakugawira acite ndi mtima woona; iye wakuweruza, aweruze ndi cangu; iye wakucita cifundo, acite ndi kukondwa mtima. (Aroma 12:6,8)

Kudandaulira ndi kuthekera kwapadera kotha kukhala chifupi ndi munthu ndi cholinga chofuna kupereka uphungu malinga ndi mau a Mulungu. Kudandaulira ndi kumatanthauza kumuitanira munthu pambali ndi choling chomupats uphungu, kumulimbikitsa kapena kupereka chilimbikitso.

Kudandaulira ndi kuthekera kopereka uphungu wanzera wauzimu. Anthu amene ali ndi mphatso imeneyi amapereka mau a chilimbikitso, chithonhozo kotero kuti anthu ena amathandizika. Malingana ndi masiku ano, tikhoza kunena kuti kudandaulira ndi chimodzimodzi ndi kupereka uphungu.

Kudandaulira kunali gawo limodzi la utumiki wa mtumwi Paulo pamene amayendera mipingo:

Pamene analalikira Uthenga Wabwino pamudzipo, nayesa ambiri akuphunzira, anabwera ku Lustra ndi Ikoniyo ndi Antiokeya, nalimbikitsa mitima ya akuphunzira, nadandauliraiwo kuti akhalebe m'cikhulupiriro, ndi kuti tiyenera kulowa m'ufumu wa Mulungundi zisautso zambiri. (Macitidwe 14:21-22)

Baibulo limafotokoza mmene kundaulira kuyenera kuchitikira:

NGATI MMENE ANGACHITIRE NDI MWANA WAKE:

monga mudziwa kuti tinacitira yense wa inu pa yekha, monga atate acitira ana ace a iye yekha, ndi kukudandaulirani, ndi kukusangalatsani ndi kucita umboni, (Atesalonika 2:11)

POPEREKA MALANGIZO MOLEZA:

lalikira mau; cita nao pa nthawi yace, popanda nthawi yace; tsutsa, dzudzula, cenjeza, ndi kuleza mtima konse ndi ciphunzitso. (2 Timoteo 4:2)

MOGWIRIZANA NDI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA:

wogwira mau okhulupirika monga mwa ciphunzitso, kuti akakhoze kucenjeza m'ciphunzitso colamitsa, ndi kutsutsa otsutsana naye. (Tito 1:9)

NDI ULAMULIRO:

Izi lankhula, ndipo ucenjeze, nudzudzule ndi ulamuliro wonse. Munthu asakupeputse.

(Tito 2:15)

KAWIRIKAWIRI PAMENE CHIMALIZIRO CHAYANDIKIRA.

osaieka kusunkhana kwathu pamodzi, monga amacita ena, komatu tidandaulirane, ndiko koposa monga momwe muona tsiku lirikuyandika. (Ahebri 10:25)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Baibulo limafotokoza za anthu ambiri amene anali ndi mphatso yadandaulira ndi kulangiza anthu ena. Werengani ma vesi awa ndi cholinga choti muonenjezere chidziwitso chanu cha mphatso zimenezi:

-Barnaba: Machitidwe 11:22-24

-Yudasi and Sila: Machitidwe 15:32

-Paulo: Machitidwe 14:22, II Akokorinto 9:5, I Atesalonika 4:1

-Yuda: Yuda 3

Kodi ndi khalidwe liti limene munthu odandaulira ayenera kuonetsera kwa munthu omudandaulira. Werengani I Atesalonika 2:11 ndi 5:14.

Pamene anthu adandauliridwa, ndi zinthu ziti zimene anthu anali kukumbuikitsidwa kuti achite?

I Petro 5:1-2 _____

II Timoteo 4:1-4 _____

I Tesalonika 2:11-12 _____

II Tesalonika 3:12 _____

Werengani ma vesi awa ndipo malizani kuyankha mafunso awa:

	Ndani	Anadandaulira ndani
Machitidwe 14:21-22	_____	_____
Machitidwe 16:40	_____	_____
Machitidwe 20:1	_____	_____
II Akorinto 1:3-7	_____	_____

MAU A NZERU

Pakuti kwa mmodzi kwapatsidwa mwa Mzimu mau a nzeru; koma kwa mnzace mau a cidziwitso, monga mwa Mzimu yemweyo: (I 1 Akorinto 12:8)

Mau a mzeru ndi kukhala ndi kuthekera kogwiritsa ntchito chidziwitso chimene chimatha kugwiritsidwa ntchito pothana ndi mavuto kapena zosowa zatsiku ndi tsiku. Anthu amene ali ndi mphatso ya nzeru amatha kugwiritsa ntchito mphatso yawo pothana ndi vuto lina lilironse kapena kupereka mayankho.

Mau a mzeru ndi kuthekera kotha kuona zinthu kapena nyengo za anthu mosiyana ndi mmene anthu ena angazionere. Izi ndi nzeru za Mulungu zimene zimagwira ntchito limodzi ndi kumvetsetsa kwa nyengo zimene anthu akudutsamo. Mpatso ya mzeru ndi kachidutswa chabe ka mzeru za Mulunguz opanda malire.

kuti itonthozeke mitima yao, nalumikizike pamodzi iwo m'cikondi, kufikira cuma conse ca cidzalo ca cidziwitso, kuti akazindikire Iwo cinsinsi ca Mulungu, ndiye Kristu, amene zolembera zonseza nzeru ndi cidziwitso zibisika mwa iye. (Akolose 2:2-3)

koma kwa iwo oitanidwa, ndiwo Ayuda ndi Ahelene, Kristu 1 mphamvu ya Mulungu, ndi 2 nzeru ya Mulungu. Koma kwa iye muli inu mwa Kristu Yesu , 7 amene anayesedwa kwa ife nzeru ya kwa Mulungu, ndi cilungamo ndi ciyeretso ndi ciombolo; (1 Akorinto 1:24,30)

Mzeru ya Mulungu ndi yosiyana ndi mzeru yadziko lapansi:

Koma mukakhala nako kaduka kowawa, ndi cotetana m'mtima mwanu, musadzitamandira, ndipo musamanama potsutsana naco coonadi. Nzeru iyi, sindiyo yotsika kumwamba, komatu iri ya padziko, ya cifuniro ca cibadwidwe, ya ziwanda. Pakuti pomwe pali kaduka ndi zotetana, pamenepo pali cisokonekero ndi cocita coipa ciri conse. Koma nzeru yocokera kumwamba iyamba kukhala yoyera,

nikhalanso yamtendere, yaulere, yomvera bwino, yodzala cifundo ndi zipatso zabwino, yopanda tsankhu, yosadzikometsera pamaso. (Yakobo 3:14-17)

Ngati mulibe mphatso ya mau a mzeru, ndi zotheka kukuza mzeru kapena luntha lanu. Mukhoza kuonjezera nzeru zanu powerenga mau a Mulungu.

ndi kuti kuyambira ukhanda wako wadziwa malembo opatulika, okhoza kukupatsa nzeru kufikira cipulumutso, mwa cikhulupiriro ca mwa Kristu Yesu. (Timoteo 3:15)

Mukhoza kupempha nzeru kwa Mulungu.

Pamenepo cilakolakoco citaima, cibala ucimo; ndipo ucimo, utakula msinkhu, ubala imfa. (Yakobo 1:15)

Pakuti Yehova apatsa nzeru; Kudziwa ndi kuzindikira kuturuka m'kamwa mwace; Iye asungira oongoka mtima nzeru yeniyeni; Ndiye cikopa ca oyenda molunjika; (Miyambi 2:6-7)

Muyenera kuzindikira kuti mzeru yauzimu imapezeka ndi wina aliyense amene ndi okhulupirira. Koma izi sizimatanthauza kuti wina aliyense ali ndi mphatso ya nzeru. Mau a nzeru ndikuthekera kumene kumaperekedwa ndi Mulungu kudzera mwa Mzimu Woyera.

ZOONJZERA POPHUNZIRA

Werengani ndime za Paulo zokhudza Mzeru: I Akorinto 2:1-13. Kodi pali kusiyana kwanji pakati pa mzeru ziwiri zimene walemba. Mtumwi Petro naye amagwiritsa ntchito mzeru mmoyo wake. Werengani: II Petro 3:15-16; I Akorinto 2:4-8.

Mzeru ikuonekera mu utumiki wa Stefano: Machitidwe 6:3,10

Mfumu Solomoni ndi chitsanzo chabwino cha Mzeru Muchipangano chakale.

Werengani buku la Miyambo limene linalembedwa ndi Solomoni. Ili ndi Buku limene limafotokoza kagwiritsidwe ntchito ka mzeru.

Werengani buku la Yakobo 3:17 ndipo tchulani makhalidwe a mzeru ya umulungu.

Werengani zitsanzo za mmene mau a mzeru amagwilira ntchito:

-Luka 2:40-52; 21:15

-Machitidwe 5:26-33

(Lingalirani mau awa "Tiyener kumvera Mulunguosati munthu").

-Deterenome 34:9

-Ekisodo 36:1-2

MAU ACHIDZIWITSO

Pakuti kwa mmodzi kwapatsidwa mwa Mzimu mau a nzeru; koma kwa mnzace mau a cidziwitso, monga mwa Mzimu yemweyo: (1 Akorinto 12:8)

Mau a chidziwitso ndikuthekera kotha kumvetsetsa zinthu zimene anthu ena sakudziwa ndipo sangamvetsetse kenako ndikugawana nawo chiidziwitso cha zinthu zimene samadziwa mothandizidwa ndi Mzimu Woyera. Mphatso yachidziwitso ndi gawo lochepa chabe la chidziwitso chonse cha Mulungu.

Gwero la chidziwitso chazimu ndi Mulungu:

amene zolemera zonseza nzeru ndi cidziwitso zibisika mwa iye. (Akolose 2:3)

Koma zonse izi acita Mzimu mmodzi yemweyo, nagawira yense payekha monga afuna. Pakuti monga thupi liri limodzi, nilikhala nazo ziwalo zambiri; koma ziwalo zonse za thupilo, pokhala zambiri, ziri thupi limodzi; momwemonso Kristu. Pakutinso mwa Mzimu mmodzi ife tonse rinabatizidwa kulowa m'thupi limodzi, ngakhale Ayuda, ngakhale Ahelene, ngakhale akapolo, ngakhale mfulu; ndipo tonse tinamwetsedwa Mzimu mmodzi. Pakutinso thupisilikhala ciwalo cimodzi, koma zambiri. (1 Akorinto 12:11-14)

Mphatso ya mau achidziwitso ndi chidziwitso chovumbulutsidwa ndi Mulungu kapena kuti ndi chidziwitso chimene chimaonetseredwa ndi Mulungu. Ichi sichidziwitso chimene mungachipeze kudzera mumaphunziro kapene kudzera mukuwerenga.

Pamene Yesu anafunsa Petro funso lauzimu, Iye anayankha ndi mau achidziwitso. Ndipo Yesu anati:

Ndipo Yesu anayankha iye, nati, Ndiwe wodala, Simoni Bar-Yona: pakuti thupi ndi mwazi sizinakuululira ici, koma Atate wanga wa Kumwamba. (Mateyu 16:17)

Mau achidziwitso ayenera kugwiritsidwa ntchito modzichepetsa chifukwa gwero lake si unuyo koma Mulungu.

Koma za zoperekedwa nsembe kwa mafano: Tidziwa kuti tid naco cidziwitso tonse. Cidziwitso citukumula, koma cikondicimangirira. Ngati wina ayesa kuti adziwa kanthu sanayambe kudziwa monga ayenera kudziwa. (1 Akorinto 8:1-2)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA:

Zitsanzo za mau achidziwitso zimene mukhoza kugwiritsa ntchito popitiriza kuphunzira ndi izi.

-Yesu:	Yohane 1:48; 4:17-18; 11:14
-Simoni:	Luka 2:25-35
-Ananiya and Safira:	Machitidwe 5:1-11
-Paulo:	Machitidwe 27:13-44
-Petro:	Machitidwe 5:1-10; 8:23; 10:19
-Ananiya:	Machitidwe 9:1

Werengani ndime zimene za izi:

-Amadziwa kumene kunali Paulo:	Vesi 11
-Amadziwa kuti amapemphera:	Vesi 11
-Amadziwa kuti anali ndi masomphenya:	Vesi 12
-amadziwa kuti anali chotengera chosankhidwa:	Vesi 15
-amadziwa kuti adzakumana ndi chizuzo:	Vesi 16
-Amadziwa kuti adzakhala mboni:	Vesi 15

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera.

2. Kodi mphatso zisanu zolankhula ndi chiani?

3. Werengani mndanda oyamba wa mphatso zolankhula. Werengani tanthauzo limene laperekedwa mumndanda wachiwiri. Lembani nambala ya tanthauzo la mphatso pa mpata umene waperekedwa.

Mndanda oyamba

___ Kudandaulira

___ uneneri

___ Mau a Mzeru

___ Kuphunzitsa

___ Mau a Chidziwitso

mndanda wachiwiri

1. Kulankhula uthenga ochokera kwa Mulungukupita kwa anthu Motsogozedwa ndi Mulungu.
2. Mau achilimbikitso kapena chitonthozo.
3. Kuthekera kophunzitsa anthu ena mau a Mulungu.
4. Kumvetsetsa mmene chidziwitso chingagwiritsidwe kukonza zinthu zolakwika
- 5 kuthekera komvetsetsa zinthu zimene anthu ena sangamvetsetse

(Mayankho Amafunso Awa Ali Kumapeto Kwa Buku Ili)

CHAPUTALA 8

MPHATSO ZOTUMIKIRA ZA MZIMU.

ZOLINGA

Pamapeto paphunziro ili mukwanitsa kupanga zinthu izi:

- Kuzindikira mphatso zisanu ndi zinayi zakutumikira.
- Kusiyanitsa pakati pa mphatso ya kutumikira ndi mpatso yothandiza.
- Kusiyanitsa pakati pa mphatso yakayendetsedwe kazinthu ndi ya utsogoleri.
- Kusiyanitsa pakati pa mpatso ya chikhulupiriro ndi chipatso chachikhulupiriro.

VESI YOTSOGOLERA

ndipo amene ali yense afuna kukhala woyamba mwa inu adzakhala kapolo wa onse.

(Marko 10:44)

MAU OYAMBA

Pali mphatso zapadera zimene zimatchedwa kuti mphatso zotumikira. Mphatso zimenezi simaudindo apadera mu mpingo ofanana ndi maudindo ngati a mtumwi, mneneri kapena m'busa. Izi si mphatso zolankhula zimene munthu amayima ndi kuyamba lulankhula ndi cholinga chotumikira mau a Mulungu ku mpingo. Komanso mphatso zimene zi si zizindikiro zodabwitsa zimene zimaperekedwa pofuna kuchitira umboni choonadi.

Mphatso zisanu ndi zinayizi zimathandizira mukayendetsedwe kampingo ndipo mphatso zimenezi ndi izi:

- Mzimu wachidziwitso - kuthandizira
- Utsogoleri - kutumikira
- Kuyendetsa zinthu -Chifundo
- Chikhulupiriro - Kucheleza alendo
- Kupereka

MIZIMU YACHIDZIWITSO

Koma kwa yense kwapatsidwa maonekedwe a Mzimu kuti apindule nao. Pakuti kwa mmodzi kwapatsidwa mwa Mzimu mau a nzeru; koma kwa mnzace mau a cidziwitso, monga mwa Mzimu yemweyo: kwa wina cikhulupiriro, mwa Mzimu yemweyo; ndi kwa wina mphatso za maciritso, mwa Mzimu mmodziyo; ndi kwa

wina macitidwe a mphamvu; ndi kwa wina cinenero; ndi kwa wina cizindikiro ca mizimu; kwa wina malilime a mitundu mitundu; ndi kwa wina mamasulidwe a malilime. (1 Akorinto 12:7-10)

Mizimu yachidziwitso ndi kuthekera kotha kuzindikira chiphunzitso, anthu ngakhale nyengo zimene ngati zili zochokera kwa Mulungu kapena kwa Satana. Tikuyenera kusiyanyitsa pakati pa mzimu wachidziwits ndi mzimu odziwa kusanthula zinthu. Mphatso imeneyi ndi yauzimu kotero kuti zinthu zauzimu zimazindikiridwa ndi zinthu zauzimunso osati ndi maganizo athu akuthupi.

Koma iye amene ali wauzimu ayesa zonse, koma iye yekha sayesedwa ndi mmodzi yense. (1 Akorinto 2:15)

Mphatso yachidziwitso ndi yapaderadera chifukwa imakhudzana kwambiri ndi kuzindikira mizimu osati chidziwitso cha chinthu china chilichonse. Mphatso imeneyi imathandiza mpingo pozindikira anthu amene akhoza kusokoneza chiyanjano cha mumpingo chifukwa zolinga zawo zolakwika, ziphunzitso zawo zabodza ndi machitidwe a zinthu osakhala bwino.

Mizimu yachidziwitso ndi yofunika chifukwa chakuti adani amene timamenyana nao saoneka ndi maso. Iwo akhoza kuzindikiridwa bwino pogwiritsa ntchito mphatso yachidziwitso.

Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba. (Aefeso 6:12)

Njira imodzi imene Satana amagwiritsa ntchito ndi chinyengo. Chifukwa cha ichi ndi zofunika kukhala ndi mphatso yachidziwitso.

Ndipo kulibe kudabwa; pakuti Satana yemwe adzionetsa ngati mngelo wa kuunika. Cifukwa cace sikuli kanthu kwakukuru ngatinso atumiki ace adzionetsa monga atumiki a cilungamo; amene cimariziro cao cidzakhala monga nchito zao. (2 Akorinto 11:14-15)

Pamene tayandikira kubweranso kwachiwiri kwa Yesu, mzimu wachinyengo udzachuluka;

Koma Mzimu anena monenetsa, kuti m' masiku otsiriza ena adzataya cikhulupiriro, ndi kusamala mizimu yosoceretsa ndi maphunziro a ziwanda, (1 Timoteo 4:1)

Mtumwi Petro anachenjeza:

Koma padakhalanso pakati pa anthuwo aneneri onama, monganso padzakhala aphunzitsi onama pakati pa inu, amene adzalowa nayo m'tseri mipatuko yotayikitsa, nadzakana Ambuye amene adawagula, nadzadzitengera iwo okha citayiko cakudza msanga. Ndipo ambiri adzatsata zonyansa zao; cifukwa ca iwo njira ya coonadi idzanenedwa zamwano. (2 Petro 2:1-2)

Ngati mulibe mphatso yachidziwitso, sindiye kuti mulibe chitetezo chili chonse. Mulungu wapereka njira imene tikhoza kuyesera mizimu. Ndipo njira imeneyi imagwira ntchito posatengera kuti muli ndi mphatso yachidziwitso kapena kuti mulibe.

Okonedwa, musamakhulupirira mzimu uli wonse, koma yesani mizimu ngati icokera mwa Mulungu: popeza aneneri onyenga ambiri anaturuka kulowa m'dziko lapansi. M'menemo muzindikira Mzimu WI Mulungu: mzimu uli wonse umen ubvomereza kuti Yesu Kristu ana dza m'thupi, ucokera mwa. Mulungundipo mzimu uli wonse umen subvomereza Yesu sucokera kwa Mulungu; ndipo uwu ndiwo mzirm wa wokana Kristu umene mudamvi kuti ukudza; ndipo ulimo m'dziko lapansi tsopano lomwe, (1 Yohane 4:1-3)

Mukhoza kugwiritsa ntchito chidziwitso chanu chazimu pofuna kudziwa chabwino ndi choipa. Ndipo chidziwitso chimenechi chimakula pamene muwerenga mau a Mulungu.

Pakuti yense wakudya mkaka alibe cizolowezi ca mau a cilungamo; pakuti ali khanda. Koma cakudya cotafuna ciri ca anthu akulu misinkhu, amene mwa kucita nazo anazoloweretsa zizindikiritso zao kusiyanyitsa cabwino ndi coipa. (Ahebri 5:13-14)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA:

Zitsanzo zili munsizi zikuonetsera kagwiritsidwe ka mphatso ya chidziwitso.

-Yesu: Mateyu 16:21-23; Yohane 1:47; Luka 9:55

-Paulo: Machitidwe 13:6-12; 16:16-18

-Petro: Machitidwe 5:1-11; 8:18-24.

(Malingana ndi Machitidwe 8:18 -24, kodi cholinga chogwiritsa ntchito mphatso yachidziwitso cha mizimu ndi chiani?)

UTSOGOLOERI:

Ndipo pokhala ife ndi mphatso zosiyana, monga mwa cisomo copatsidwa kwa ife, kapena mphatso yakunenera, tinenere monga mwa muyeso wa cikhulupiriro; kapena iye wakudandaulira, kukudandaulirako; wakugawira acite ndi mtima wooka; iye wakuweruza, aweruze ndi cangu; iye wakucita cifundo, acite ndi kukondwa mtima. (Aroma 12:6,8)

Mphatso yautsogoleri ndi kuthekera kokhazikitsa zolinga pa utumiki zogwirizana ndi Mulungu. Komanso munthuyo amatha kufotokozera zolinga zimenezi kwa anthu ena. Munthu amene ali ndi mphatso yautsoyi amatha kukopa anthu ena kuti akwaniritse zolinga zimene zakhazikitsidwa ndi cholinga chofuna kubweleretsa ulemelero kwa Mulungu.

Munthu amene ali ndi mphatso yautsogoleri ayenera kukwanitsa kutsogolera banja lake.

Koma ngati munthu sadziwa kuweruza nyumba ya iye yekha, adzasunga bwanji Mpingo wa Mulungu? (1 Timoteo 3:5)

Okhulupirira ayenera kupereka ulemu kwa anthu amene ali atsogoleri mumpingo.

Koma, abale, tikupemphani, dziwani iwo akugwiritsa nchito mwa inu, nakhala akulu anu mwa Ambuye, nakuyatnibirani inu; ndipo muwacitire ulemu woposatu mwa cikondi, cifukwa ca nchito yao. Khalani mumtendere mwa inu nokha. (Atesalonika 5:12-13)

Tikuzidwa kuti:

Mverani atsogoleri anu, nimuwagonjere; pakuti alindirira moyo wanu, monga akuwerengera; kuti akacite ndi cimwemwe, osati mwacisoni: pakuti ici sicikupindulitsani inu. (Ahebri 13:17)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA:

Anthu atatu amene anali amphamvu anali Mose, Yoswa, ndi Davide. Nkhani ya Davide imapezeka mabuku a Eksodo ndi Deteronome. Pamene nkhani ya Yoswa ikupezeka mu buku la Yoswa. Mukhoza kuwerenfa nkhani yokhudza Davide kuchokera mu buku la II Samueli.

Atsogoleri ena amphamvu anali:

- Nehemiya Buku la Nekemiya
- Ezara Buku la Ezara ndi Nehemiya
- Petro Buku la machitidwe.

KAYENDETSSEDWE KA ZINTHU

Ndipotu Mulungu anailea ena m'Eklesia, poyamba arumwi, aciwiri aneneri, acitatu aphunzitsi, pamenepo zozizwa, pomwepo mphatso zamaciritso, mathandizo, maweruziro, malilime a mitundu mitundu. (1 Akorinto 12:28)

Malingana ndi Baibulo, munthu amane ali ndi mphatso ya kayandetsedwa kazinthu amakhala kuti ali ndi kuthekera kopereka chitsogozo komanso kupanga ziganizo mmalo mwa anthu ena. Tanthauzo la kayendetsedwe ka zinthu ndi chimodzimidzi mmene munthu oyendetsa sitima amaangolera sitimayo kuti iyende.

Okhala m'Zidoni ndi Arivadi ndiwo opalasa ako; anzeru ako, Turo, okhala mwa iwe, ndiwo oongolera ako. (Ezekieli 27:8)

Munthu amene ali ndi mphatso imeneyi udindo wake ndikupereka chitsogozo komanso kupanga ziganizo mmalo mwa munthu wina. Oyendetsa sitima sikuti sitimayo imakhala kuti ndi yake, koma iye amakhala kuti wapatsidwa udindo oti awongolere sitimayo kufikira itafika kumene ikufuna kukafika.

Mphatso yautsogoleri ndi yakayendetsedwe kazinthu imakhazikika pa luso lakayendetsedwe ka zinthu ndi cholinga chofuna kukwaniritsa zolinga zauzimu. Nthawi zambiri okhulupirira

amakhala ndi mphatso ya utsogoleri komanso ya kayendetsedwe kabwino ka zinthu. Koma ngati munthu ali ndi mphatso imodzi mwamphatso ziwiri zimenezi ndiye kuti ayenera kugwiritsa ntchito anthu ena amene ali ndi mphatso imene iye alibe.

Munthu amene ali ndi mphatso yakayendetsedwe ka zinthu akhoza kupereka chitsogozo komanso kupanga ziganizo mmalo mwa anthu ena. Koma ngati munthuyu alibe mphatso yautsogoleri ndiye kuti alibe kuthekera kotha kuwakopa anthu kuti anthu akagwire naye ntchito ndikukwaniritsa zolinga zimene iye ali nazo.

Nthawi zambiri aphunzitsi ndi abusa amakhala ndi mphatso yautsogoleri. Amatha kuwakopa anthu kuti athe kukwaniritsa zolinga zuazimu. Koma ambiri mwa iwo alibe mphatso yakayendetsedwe ka zinthu. Ngakhale kuti ali ndikuthekera kotha kuwakopa anthu koma iwo nthawi zambiri amakhala opanda kuthekera kotha kuyendetsa zinthu mwa iwo okha.

Ubale umene unalipo pakati pa Paulo ndi Tito umaonetsera mmene mphatso yakayendetsedwe kazinthu imagwilira ntchito. Kupatula mphatso zina zimene Paulo anali nazo, iye analinso ndi mphatso ya utumwi. Iye anadzala mpingo ku dera la creta koma Tito anathandiza mukayendetsedwe ka mpingou.

Cifukwa ca ici ndinakusiya iwe m'Krete, kuti ukalongosole zosowa, nukaike akuru m'midzi yonse, monga ndinakulamulira; (Tito 1:5)

Paulo anasankha Tito kuti ayendetse mipingo imene anadzala ku Creta. Ngakhale kuti Paulo anali ndi Ulamuliro mumipingo yonse, Tito anali ndi udinto oyendetsa zinthu mogwirizana ndi uphungu ochokera kwa Paulo. Malingana ndi ndime imeneyi, ntchito imodzo ya munthu oyendetsa zinthu ndi kuphunzitsa anthu ena kuti atenge maudindo autsogoleri mumpingo.

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Werengani vuto limene likufotokozedwa pa Machitidwe 6:1-7. Kodi limeneli ndi vuto lanji? Kodi ndi ndani amene anagwiritsa ntchito mphatso ya utsogoleri? ndipo ndi ndani amene anakatha kukhala ndi mphatso ya utsogoleri?

Werengani Luka 14: 28-30 ndipo onana kufunika kokhala ndi dongosolo la zinthu komanso kayendetsedwe kabwino kazinthu.

Werengani zokhudza moyo wa Yosefe pa Genesis 37 ndi 50. Iye anayendetsa ndi kutsogolera zinthu mmalo mwa Farao. Werenganinso Machitidwe 7:9-10.

CHIKHULUPIRIRO

Koma kwa yense kwapatsidwa maonekedwe a Mzimu kuti apindule nao: kwa wina cikhulupiriro, mwa Mzimu yemweyo; (1 Akorinto 12:7-9)

Munthu amene ali ndi mphatso yachikhulupiriro ali ndi kuthekera kwapadera kokhala ndi cikhulupiriro mwa Mulungunga khale munyengo zovuta. Anthu amene ali ndi mphatso

imeneyi amakhala ndi kulimbika mtima kuti Mulungu achitapo kanthu ngakhale anthu ena asakuhulupirira. Baibulo limafotoza za chikhulupiriro motere:

Koma cikhulupiriro ndico cikhazikitso ca zinthu zoyembekezeka, ciyesero ca zinthu zosapenyeka. (Ahebri 11:1 1)

Chikhulupiriro chimapereka chiyembekezo cha malonjezano a mtsogolo kuti ndi owonadi ngakhale kuti ndi osaoneka koma ndi enieni.

Pali mitundu ingapo ya chikhulupiriro. Pali chikhulupiriro chachilengengedwe chimene chimakhudza kukhulupirira zinthu zimene ndi zokhazikika kale. Baibulu limafotokozanso za chikhulupiriro chopaturidwa (Agalatiya 2:20) chikhulupiriro chodziteteza (Aefeso 6:16) komanso chikhulupiriro chopulumutsa (Aroma 5:1)

Baibulo limafotokoza kuti pali mlingo osiyanasiyana wachikhulupiriro. Yesu anafotokoza za anthu amene samagwiritsa chikhulupiriro chao ngati anthu opanda chikhulupiriro. (Mateyu 17:17). Iye anakambanso za anthu a chikhulupiriro chochepa. (6:30; 8:26:1431 Luke 12:28). Anakambaso za anthu achikhulupiriro chachikulu.

Baibulo limafotokoza kuti wina aliyense ali ndi mlingo wina wake wachikhulupiriro umene unaperekedwa ndi Mulungu ngati mphatso (Aroma 12:3b) Komanso Baibulo limatsindika kuti timapulumsidwa ndi chikhulupiriro (Aefeso 2: 8) Pamene mphatso ya chikhulupiriro ndi kuthekera kwa padera kotha kukhulupirira Mulungumu gawo lina lilironse la moyo. Ichi ndi chichikhulupiriro chimene sichimaika malire pa Mulungukomanso ndi chikhulupiriro chimene sichimakhala ndi zinthu zosatheka.

Comweco cikhulupiriro cidza ndi mbiri, ndi mbiri idza mwa mau a Kristu.

Aroma 10:17

Chikhulupiriro ndi chimodzi mwachipatso cha Mzimu komanso chipatso ya Mzimu Woyera. Chikhulupiriro ngati chipatso chauzimu ndi mphamvu pamene chipatso ndi chikhalidwe chimene munthu amaonetsera. Chikhulupiriro ngati mphatso chikhoza kufotokozeredwa ngati zinthu zimene munthu amaonetsera. Chikhulupiriro ndi mmene munthu amaonera zinthu ndipo chikhoza kukula ngati mmene chipatso chinachilichonse chakuthupi chimakulira.

ZOONJEZERA POPHUNZIRA:

Werengani Ahebri 11. Chaputala ichi chikupereka zitsanzo za anthu amene anali ndi chikhulupiriro chachikulu. Lembana mndanda wa zinthu zimene anthu awa anakwaniritsa chifukwa chachikhulupiriro.

- Abrahamu anatchedwa munthu wachikhulupiriro: Aroma 4:16-21; Ahebri 11:18-19
- Stefano anali ndi mphatso yachikhulupiriro: Machitidwe 6:5-8
- Banaba naye anali ndi chikhulupiriro: Machitidwe 11:22-24

-Paulo anaonetsera chikhulupiriro chachikulu: Machitidwe 27.

-Chikhulupiriro chimatsindika zinthu zimene ndi zosatheka: I Akorinto 13:2

KUPEREKA

Ndipo pokhala ife ndi mphatso zosiyana, monga mwa cisomo copatsidwa kwa ife, kapena mphatso yakunenera, tinenere monga mwa muyeso wa cikhulupiriro; kapena iye wakudandaulira, kukudandaulirako; wakugawira acite ndi mtima woota; iye wakuweruza, aweruze ndi cangu; iye wakucita cifundo, acite ndi kukondwa mtima. (Aroma 12:6,8)

Munthu amene ali ndi mphatso yopereka ali ndi kuthekera kopereka zinthu kapena ndalama zimene ku ntchito ya ambuye. Anthu oterewa amachita izi ndi chimwemwe. Kupereka zinthu ngati nthawi, mphamvu zathu komanso luso lathu ndi gawo limodzi la mphaso yakupereka. Mfundo imodzi yokhudza kupereka ndi yakuti kupereka kumachitika mwa ufulu.

Akhristu onse ayenera kupereka ku ntchito ya Mulungu.

Yense acite monga anatsimikiza mtima, si mwa cisoni kapena mokakamiza, pakuti Mulunguakonda wopereka mokondwerera. (2 Akorinto 9:7)

Okhulupirira onse akuyenera kupereka chakhumi kuchokera ku chuma chao. Chakhumi ndi magawo khumi a chuma chathu. Ngati okhulupirira sapereka chakhuma ndi chimodzimodzi kumubera Mulungu.

Mubwere nalo limodzi limodzi lonse la khumi, ku nyumba yosungiramo, kuti m'nyumba mwanga mukhale cakudya; ndipo muniyese nako tsono, ati Yehova wa makamu, ngati sindikutsegulirani mazenera a kumwamba, ndi kukutsanulirani mdalitso wakuti adzasoweka malo akuulandira. Ndipo ndidzadzudzula zolusa cifukwa ca inu, kuti zisakuonongerani zipatso za nthaka yanu; ngakhale mpesa wanu sudzayoyoka zipatso zace, zosaca m'munda, ati Yehova wa makamu. Ndipo amitundu onse adzacha inu odala; pakuti mudzakhala dziko lokondweretsa, ati Yehova wa makamu. (Malaki 3:10-12)

Malingana ndi ndime imeneyi, anthu amene amapereka akulonjezedwa:

1. Madalitso osefukira kwambiri vesi 10.
2. Mulungu adzadalitsa ntchito imene imabweretsa chuma vesi 11.
3. Adzakhala mdalitso kumafuko onse adziko lapansi vesi 12
4. Nthaka yawo idzadalitsidwa.

Mulungu amadalitsa munthu kuchuma malingana ndi mmene iye amaperekera. Iye amapereka ndi cholinga choti muthe kupereka kuntchito ya ambuye.

Koma nditi ici, kuti iye wakufesa mouma manja, mouma manjanso adzatuta. Ndipo iye wakufesa moolowa manja, moolowa manjanso adzatuta. Ndipo Mulunguakhoza

kucurukitsira cisomo conse kwa inu; kuti inu, pokhala naco cikwaniro conse m'zinthu zonse, nthawi zonse, mukacurukire ku nchito yonse yabwino; (Akorinto 9:6,8)

Yesu naye analonjeza kuti:

Patsani, ndipo kudzapatsidwa kwa inu; muyeso wabwino, wotsendereka, wokucumuka, wosefukira, anthu adzakupatsani m'manja mwanu. Pakuti 7 kudzayesedwa kwa inu ndi muyeso womwewo muyesa nao inu. Mmene mungapezera ndalama kapena zinthu zikufotokozeredwa mu Buku la Aefeso: (Luka 6:38 6)

Wakubayo asabenso; koma makamaka agwiritse nchito, nagwire nchito yokoma ndi manja ace, kuti akhale naco cakucereza wosowa. (Aefeso 4:28)

Paulo akuyankhula zakupereka pakati pa okhulupirira aku Filipo:

Koma ndiri nazo zonse, ndipo ndisefukira; ndadzazidwa, popeza ndalandira kwa Epafrodito zija zidacokera kwanu, mnunkho wa pfungo labwino, nsembe yolandirika, yokondweretsa Mulungu. (Afilipi 4:18)

Iye akufotokoza kuti chifukwa chakuti kupereka kwao kunali ngati nsembe, iwo anamkondweretsa Mulungu. Ndipo iye anauza okhulupirirawo kuti:

Koma Mulunguwanga adzakwaniritsa cosowa canu ciri conse monga mwa cuma cace m'ulemerero mwa Kristu Yesu. (Afilipi 4:19)

Malonjezano awa anaperekedwa kwa anthu amene anapereka ku ntchito ya Mulungu.

Kumbukirani kuti ngakhale kuti okhulupirira onse ayenera kupereka ndikudalitsidwa chifukwa chakupereka, koma munthu amene ali ndi mpatso yakupereka amakhala ndi kuthekera kodabwitsa kopereka mokondwera. Anthu oterewa amakhala ndi zolinga zauzimu pamene apereka.

ZOONJERA POPHUNZIRA:

Munsimu muli zitsanzo za m, Baibulo za anthu amene anali ndi kuthekera kodabwitsa kopereka kwa Mulungu. Ndi zotheka kuti anthu amenewa anali ndi mpatso yauzimu yopereka.

-Mzimayi wamasiye: Marko 12:41-44; Luke 21:1-4

-Mariya: Yohane 12:3-8

-Mpingo waku Agalatiya: Agalatiya 4:15

-Mpingo waku Afilipo: Afilipo 4:10-18

- Mpingo waku Makedoniya: II Akorinto 8:1-7

Kodi ndi cholinga chanji chimene anthu ayenera kupereka? Werengani Mateyu 6:3 ndi Aefeso 4:28: I Akorinto 13:3.

Ndipotu Mulungwanailea ena m'Eklesia, poyamba arumwi, aciwiri aneneri, acitatu aphunzitsi, pamenepo zozizwa, pomwepo mphatso zamaciritso, mathandizo, maweruziro, malilime a mitundu mitundu. 1 Akorinto 12:28

KUTHANDIZIRA:

Munthu amene ali ndi mphatso yothandizira ali ndi kuthekera kothandiza anthu ena kuti atumikire Mulungu moyenenelera. Munthu wina aliyense amene amathandizira mu mpingo tikhoza kunena kuti ali ndi mphatso yothandizira. Pamene Paulo anatomiza mlongo Febe kuti apite ku Roma, Iye anapempha okhulupirira kuti anhandize Febe ndi mphatso zapadera.

Ndipereka kwa inu Febe, mlongo wathu, ndiye mtumiki wamkazi wa Mpingo wa Ambuye wa ku Kenkrey; kuti mumlandire iye mwa Ambuye, monga kuyenera oyera mtima, ndi kuti mumthandize m'zinthu zili zonse adzazifuna kwa inu; pakuti iye yekha anali wosungira ambiri, ndi ine ndemwe. Aroma 16:1-2

Priska ndi Akula anatomikira Paulo ndi mphatso yawo yothandizira. Ndipo Paulo analemba:

Mulankhule Priska ndi Akula, anchito anzanga m'Kristu Yesu, (Aroma 16:3)

Mphatso yothandizira ndi ntchito ina iliyonse imene imathandizira munthu wina kapena kuti zili ngati kutumikira ngati munthu othandizira.

ZOONJEZERA POPHUNZIRA:

- Tabita anali ndi mphatso yothandiza: Machitidwe 9:36
- Azimayi anathandiza Yesu Khristu mu utumiki wake. Marko 15:40-41:
- Thandizo limene lingaperekedwe likhoza kukhala mu gawo lakayendetsedwe kazinthu
- Eksodo 18:22; Numeri 11:17
- Utumiki othandizira ukhoza kuthandizira anthu amene ndi ofooka: Machitidwe 20:35.

KUTUMIKIRA:

Ndipo pokhala ife ndi mphatso zosiyana, monga mwa cisomo copatsidwa kwa ife, kapena mphatso yakunenera, tinenere monga mwa muyeso wa cikhulupiriro; kapenayakutumikira, tidzipereke ku utumiki uwu; kapena iye wakuphunzitsa, kukuphunzitsako; (Aroma 12:6-7)

Mphatso yakutumikira ndi kuthekera kotha kugwira ntchito zautimiki zimene ziyenera kugwiridwa. Munthu otumikira amatumikira anthu ena ndi cholinga choti akwaniritse zolinga zao zauzimu powapepuza pa zinthu zina zimene amayenera kuchita.

Kutumikira kumasiyana ndi kuthandiza chifukwa chakuti kutumikira kumamupepuza munthu amene ameyenera kuchita kapena kukwaniritsa udindo wina wake. Munthu amene akutumikira ametenga udindo ndi cholinga chopepuza anthu kuti athe kugwiritsa ntchito mphatso yao.

Pamene munthu amene ali ndi mphatso yothandizira amathandiza munthu wina kuti akwaniritse kuchita utumiki. Mwachitsanzo, anthu oyimba amathandiza m'busa kuti akwaniritse udindo wake nthawi yachipembedzo. Anthuwa amakhala kuti akuthandiza kuti munthu wa Mulunguakwanitse udindo wake osati kumulandira m'busayu udindo wake.

Koma ndi zotheka kutinso munthu amene ali ndi mphatso yotumikira akhoza kumulandira m'busa kuti asatenge gawo logawa chakudya kwa anthu osowa mu mpingo. Chitsanzo chabwino chimapezeka mumpingo oyamba pamene anthu ena amatumikira pogawa chakudya ndi cholinga choti awapepuze atumwi pogwir ntchito imeneyi komanso ndi chilinga apereke mwayi kwa atumwi kuti akhazikike pa kuchita maudindo awo ofunika:

Koma masiku awo, pakucurukitsa ophunzira, kunauka cidandaulo, Aheleniste kudandaula pa Ahebri, popeza amasiye ao anaiwalika pa citumikiro ca tsiku ndi tsiku. Ndipo khumi ndi awiriwo anaitana unyinjira wa ophunzira, nati, Sikuyenera kuti ife tisiye mau a Mulungundi kutumikira podyerapo. Cifukwa cace, abale, yang'anani mwa inu amuna asanu ndi awiri a mbiri yahwino, odzala ndi Mzimu ndi nzeru, amene tikawaike asunge nchito iyi. Koma ife tidzalimbika m'kupemphera, ndi kutumikira mau. (Macitidwe 6:1-4)

wonani zoyenereza zimene munthu otumikira ameyenera kukhala nazo. Iwo amayenera kukhala anthu achilungamo kapena kuti owona mtima komanso odzadzidwa ndi Mzimu Woyera ndi mzeru.

Ambuye acitire banja la Onesiforo cifundo; pakuti anatsitsimutsa ine kawiri kawiri, ndipo sanacita manyazi ndi unyolo wanga; komatu pokhala m'Roma iye anandifunafuna ine ndi khama, nandipeza, (Ambuye ampatse iye apeze cifundo ndi Ambuye tsiku lijalo); ndi muja ananditumikira m'zinthu zambiri m'Efeso, uzindikira iwe bwino. (Timoteo 1:16-18)

Mphatso yakutumikira imafuna kusenya zowawa za anthu ena:

Nyamuliranani zothodwetsa, ndipo koteru mufitse cilamulo ca Kristu. (Agalatiya 6:2)

Yesu Khristu anafotokoza mmene munthu otumikira ayenera kuonera zinthu:

Ndipo anati kwa iwo, Mafumu a anthu a mitundu awacitira ufumu; ndipo iwo amene awacitira ulamuliro anenedwa, Ocitira zabwino. Koma sipadzatero ndi inu; komatu iye ali wamkuru mwa inu, akhale ngati wamng'ono; ndi iye ali woyamba, akhale ngati wotumikira. Pakuti wamkuru ndani, iye wakuseama pacakudya kapena wakutumikirapo? si ndiye wakuseama pacakudya kodi? koma Ine ndiri pakati pa inu monga ngati wotumikira. (Luka 22:25-27)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA:

Zitsanzo zakumikira:

- **Angelo** Ahebri 1:14; 4:11; Mark 1:13
- **Kugawa chakudya Yohane** 2:5,9; Luke 10:40

CHIFUNDO

Ndipo pokhala ife ndi mphatso zosiyana, monga mwa cisomo copatsidwa kwa ife, kapena mphatso yakunenera, tinenere monga mwa muyeso wa cikhulupiro; kapena iye wakudandaulira, kukudandaulirako; wakugawira acite ndi mtima wooka; iye wakuweruza, aweruze ndi cangu; iye wakucita cifundo, acite ndi kukondwa mtima. (Aroma 12:6,8)

Chifundo chimatanthauza kuonetsa kukhudzika. Izi zimasonyeza kuti munthu akutha kumvetsa mmene anthu ena akumvera. Munthu amene ali ndi mphatso ya chifundo amakhala ndi kukhudzika kwapadera ndi anthu ena amene akuvutika komanso amakhala ndi kuthekera kowathandiza anthuwo.

Mphatso yachifundo imakhudza kaonedwe kazinthu komanso machitidwe. Chitsanzo chabwino ndi nkhani ya msamariya wachifundo pa Luka 10:30-37. Msamariya sanangoonetsa kukhudzika kokha ayi, koma iye anachitaponso kanthu pothandiza munthu omenyedwa ndi achifwamba uja.

Choyenereza cha mphatso ya chifundo ndi chakuti munthu anayera kuonetsera mphatsoyi mokondwera. Mau oti mokondwera amatanthauza kukhala okonzeka kuchita zinthu mwachimwe ndi cholinga chofuna kuthandiza munthu amene akuvutika.

Siyanitsani chifundo cha ophunzira a Yesu ndi chimene Yesu anali nacho malingana ndi ndime izi:

Ndime	Yesu	Ophunzira
Mateyu 15:23-28	anachilitsa mtsikana	anamubwenza
Mzimay wa ku Surofonika		
Marko 8:1-9	Anawadyetsa	anawabwenza Chikhamu
Mateyu 20:31 -34	anawachiritsa anthu aakhungu	amafuna kuti akhale chete
Marko 10: 48-49	Anawachiritsa	amafuna kuti akhale chete Batumeyu wakhungu

ZONJEZERA POPHUNZIRA

- Machiritso a Yesu Khristu: Matthew 9:27-30; 15:21-28; 17:14-18; 20:30-34; Mark 10:46-52; Luke 17:1-14
- Msamariya wachifundo: Luka 10:30-37
- Dorika Machitidwe 9:36-42

KUCHELEZA ALENDO

mucerezane wina ndi mnzace, osadandaula: monga yense walandira mphatso, mutumikirane nayo, ngati adindo okoma a cisomo ca mitundu mitundu ca Mulungu; (1 Petro 4:9-10)

Kuchereza alendo ndi kuthekera kwa padera kumene Mulungu amapereka kwa anthu ena ndi cholinga choti akathe kupereka chakudya komanso malo ogona kwa anthu amene ndi osowa. Choyenera cha mphatso imeneyi ndi chakuti munthu ayenera kuchita zinthu izi opanda kuwiringula kapena kuti munthu ayenera kuchita opanda kukakamizidwa kapena kudandaulira.

Kuchereza alendo ndi chizindikiro chachikondi chopanda chinyengo:

Cikondano cikhale copanda cinyengo, Dana naco coipa; gwirizana naco cabwino. Patsani zosowa oyera mtima; cerezani aulendo. (Aroma 12:9,13)

Kuchereza alendo ndi chinthu chimodzi chimene chimamuyenera munthu kuti akhale mtsogoleri:

Ndipo kuyenera woyang'anira akhale wopanda cirema, wokonda kucereza alendo, wokhoza kuphunzitsa; (1 Timoteo 3:2 2)

komatu wokonda kucereza alendo, wokonda zokoma, wodziweruza, wolungama, woyera mtima, wodziletsa; (Tito 1:8)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Lidiya ndi chitsanzo chabwino cha mphatso ya kucheleza alendo: Machitidwe 16:14-15

Gaya anamuchereza Paulo mu mzinda wa Roma: Aroma 16:23.

Werengani zakuchereza alendo: Onani zimene zalembedwa pa buku la Ahebri 13: 1-2 komanso werengani nkhani ya Abrahamu ndi Sara pa Genesis 18.

MAYESO ODZIYESA NOKHA:

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

2. Tchulani zipatso zisanu ndi zinayo zotumikira:

<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>

3. Kodi ndi chifukwa chiani mphatso zimenezi zimatchedwa kuti mphatso zotumikira?

4. Kodi pali kusiyana bwanji pakati pa mphatso yautsogoleri ndi yakuyendetsa zinthu.

5. Kodi mphatso ya kuthandiza imasiyana bwanji ndi mphatso yakutumikira?

6. Werengani mndandanda wa mphatso zotumikira mu mndanda oyamba. Werengani mosamalitsa tanthauzo la mphatsozi mu mndandanda wachiwiri. Ndipo lembani nambala pa mpata imene ikufotokozerana mphatso imene yalembedwayo.

Mndandanda oyamba

mdandanda wachiwiri.

___ Kutumikira

1. Kuthekera kotha kuunikira anthu, ziphunzitso komanso nyengo
Ngati zili zochokera kwa Mulungu

___ kuthandizira

2. Kuthekera kopangits anthu ena kuti athe kukwaniritsa zolinga zawo

___ Utsogoleri

3 kutsogolera mmalo mwa anthu ena.

___ Kuyendetsa zinthu

4. Kuthekera kotha kukhululupirira zinthu.

___ Kupereka

5. Kuthekera kwapadera kotha kupereka.

___ Chifundo

6. Kuthandizira anthu ena mu utumiki.

___ mzimu wachidziwitso

7. Kuonetsera chifundo.

____ chikhulupiriro

8 Kupereka chakudya ndi malo ogona.

____ Kucheleza alendo

9 Kuthandizira anthu ena potenga maudindo awo ndi cholinga choti
apepukidwe

7. Kodi chiganizo ichi ndi cholondora kapena chabodza: Ndi okhawo amene ali ndi mpatso yakupereka amene ayenera kupereka kuntchito ya ambuye. Chiganizochi ndi:

8. Fotokozani tanthauzao la chikhulupiriro.

9. Kodi pali kusiyana kwanji pakati pa chipatso chachikhulupiriro ndi mpatso yachikhulupiriro.

10. Kodi mungakuze bwanji chikhulupiriro chanu?

(mayankho amafunso awa ali kuamapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Kupatula mphatso zimene zatchulidwazi, pali mphatso zina zimene sitinganene kuti ndi mphatso za Mzimu Woyera koma ndi mphatso zimene anthu amakhala nazo.

KUSAKWATIRA:

Kusakwatira ndi mphatso imene Mulungu amapereka kwa anthu ena ndi cholinga choti atumikire Mulungu. Pa 1 Akorinto 7:7-8 akufotokoza kuti kusakwatira chisakhakhale chinthu chokakamiza kwa munthu wina aliyese chifukwa chakuti ndi mphatso (werengani 1 Timoteo 4:1-5.) mpingo umathandizika ndi anthu amene ali ndi mphatso yosakwatira (werengani 1 Akorinto 7:32-35)

KUPEMBEDZERA

Mphatso yakupembedzera ndi kuthekera kumene Mulungu amapereka kwa anthu kuti anthe kupemphera kwa nthawi yaitali. Kupembedzera kumatanthauza kupemphelera anthu ena. Anthu opembedzera amapemphelera zosowa za anthu, utsogoleri, mautimiki komanso maiko.

Ngakhale kuti Baibulo silimatchula kuti kupembedzera ndi mphatso yauzimu, koma pali umboni kuti Mulungu anapereka kupembedzera ngati mphatso (Werengani Aroma 8:26-27). Werengani ndime zili munsimuzi ndipo pezani zolinga za pemphero lopembedzera.

-Yakobo 5:14-16 – Numeri 14:17-19

-1 Timoteo 2:1-2 – Machitidwe 7:60

-Aefeso 6:19

KUSEMASEMA.

Pali mphatso yapadera ya zosemasema. Mphatsoyi ndi kuthekera kwapadera kotha kusema zinthu zokongolora zimene zimagwira ntchito pa ntchito ya ambuye. Chitsanzo chabwino ndi anthu amene anapatsidwa ukadauro wapadera ndi cholinga choti akonze zinthu zimene zingathe kutumikira mu nyumba ya Ambuye. (Eksodo 28:3 komanso Eksodo 31: 3-6)

CHAPUTALA 9

ZIZINDIKIRO ZA MZIMU WOYERA

ZOLINGA:

Pamapeto pa phunziro ili muyenera kukwaniritsa zinthu izi.

- Kupeza zindikiro zinayi za mphatso za Mzimu Woyera.
- Kufotokoza cholinga cha zozwizwitsa.
- Kufotokoza zinthu zisanu zoyambitsa matenda akuthupi.
- Kufotokoza kusiyana pakati pa mphatso ya malirime ndi kulankhula malirime ngati chizindikiro cha ubatizo wa Mzimu Woyera.
- Kufotokoza mfundo za Baibulo za kagwiritsidwe ntchito ka mphatso ya malirime.

VESI YOTSOGOLERA:

tidzapulumuka bwanji ife, tikapanda kusamala cipulumutso cacikuru coteru? cimene Ambuye adayamba kucilankhula, ndipo iwo adacimva anatilimbikitsira ife; pocita umboni pamodzi nao Mulungunso ndi zizindikilo, ndi zozizwitsa ndi mphamvu za mitundu mitundu ndi zogawira za Mzimu Woyera, monga mwa cifuniro cace. (Ahebri 2:3-4)

MAU OYAMBA

Pali mphatso zinayi zimene zimatchedwa mphatso za zizindikiro chifukwa zimaonetsera mphatso ya Mulungu ikugwira ntchito kudzera mwa okhulupirira ngati umboni wa mau ake:

Ndipo iwowa anaturuka, nalalikiraponseponse, ndipo Ambuye anacita nao pamodzi, natsimikiza mau ndi zizindikilo zakutsatapo, Amen. (Marko 16:20)

Mphatso za zizindikiro zimaonekera mwa okhulupirira kudzera mumachiritso, zozwizwitsa komanso kupereka uthenga wapadera kudzera mumalirime. Mphatso zauzimu ndi chizindikiro kwa anthu osakhulupiriro kuti Mulungu alipo.

Zizindikiro zinayi za mphatso ndi izi:

- Zozwizwitsa
- Machiritso
- Malirime
- Kumasulira malirime

ZOZWIZWITSA

Koma kwa yense kwapatsidwa maonekedwe a Mzimu kuti apindule nao. Pakuti kwa mmodzi kwapatsidwa macitidwe a mphamvu1 (Akorinto 12:7-10)

Kudzera mwa mwa munthu amene ali ndi mphatso ya zozizwitsa, Mulungu amapanga zozizwitsa zimene ndi zinthu zimene sizingamvetsetseke kuthupi. Ichi chimakhala chizindiro choti Mulungu ali ndi mphamvu kuposa Satana.

Zozizwitsa zimakhala ndi cholinga. Mulungu amagwiritsa ntchito zozizwitsa pofuna kuchitira umboni pa uthenga Wabwino:

tidzapulumuka bwanji ife, tikapanda kusamala cipulumutso cacikuru coteru? cimene Ambuye adayamba kucilankhula, ndipo iwo adacimva anatilimbikitsira ife; pocita umboni pamodzi nao Mulungunso ndi zizindikilo, ndi zozizwitsa ndi mphamvu za mitundu mitundu ndi zogawira za Mzimu Woyera, monga mwa cifuniro cace. (Ahebri 2:3-4)

Zozizwitsa zimapangitsa anthu kuti athe kukhulupirira Uthenga Wabwino ndi kulandira moyo osatha:

Ndipo zizindikilo zina zambiri Yesu anazicita pamaso pa akuphunzira ace, zimene sizinalembedwa m'buku ili; koma zalembedwa izi kuti mukakhulupirire kuti Yesu ndiye Kristu Mwana wa Mulungu, ndi kuti pakukhulupira mukhale nao moyo m'dzina lace. (Yohane 20:30-31)

Zozizwitsa zimagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu ngati chitsikimizo cha munthu amene akutumikira Uthenga Wabwino;

Iyeyu anadza kwa Yesu usiku, nati kwa iye, Rabi, tidziwa kuti Inu ndinu mphunzitsi wocokera kwa Mulungu; pakuti palibe munthu akhoza kucita zizindikilo zimene inu mucita, ngati Mulungusakhala naye, (Yohane 3:2)

Amuna inu Aisrayeli, mverani mau awa: Yesu Mnazarayo, mwamuna wocokera kwa Mulungu, wosonyezedwa kwa inu ndizimphamvu, ndi zozizwa, ndi zizindikilo, zimene Mulunguanazicita mwa iye pakati pa inu, monga mudziwa nokha; (Macitidwe 2:22)

Mulungu anachitira umboni za utumuki wa atumwi kudzera mu zozizwitsa:

Zizindikilotu za ntumwi zinacitika pakati pa inu, ri'cipiriro conse, ndi zizindikilo, ndi cozizwa, ndi zamphamvu. (2 Akorinto 12:12)

Pali mitundu yosiyanasia ya zozizwitsa. Yesu anaoetsera ulamuliro pa zinthu zachilengedwe:

Ndipo anauka, nadzudzula mphepo, nati kwa nyanja, kuti, Tonthola, khala bata. Ndipo mphepo inaleka, ndipokunagwa bata lalikuru. (Marko 4:39)

Machiritso akuthupi ndi kuchotsa ziwanda

Ndipo Mulunganacita zamphamvu za pa zokha ndi manja a Paulo; kotero kuti anamuka nazo kwa odwala nsaru zopukutira ndi za panchito, zocokera pathupi pace, ndipo nthenda zinawacokera, ndi mizimu yoipa inaturuka. (Macitidwe 19:11-12)

Zozizwitsa zimene Paulo anachita zinatchedwa “zozizwitsa zapadera.” Izi zimatchedwa zapadera pofuna kuonetsera kuti zozizwitsa zimachitika pafupipafupi mu mpingo oyamba. Mpingo oyamba unabadwa kudzera muchionetsero cha zozizwitsa za mphamvu.

Kuchita zozizwitsa sizimatanthauza kuti munthu kapena kuti utumiki ndi ochokera kwa Mulungu. Nayenso Satana amanyenga anthu ndi zodabwitsa zake:

ndiye amene kudza kwace kuli monga mwa macitidwe a Satana, mu mphamvu yonse, ndi zizindikilo ndi zozizwa zonama; ndi m'cinyengo conse ca cosalungama kwa iwo akuonongeka, popeza cikondi ca coonadi sanacisandira, kuti akapulumsidwe iwo. Ndipo cifukwa cace Mulungu atumiza kwa iwo macitidwe a kusoceretsa, kuti akhulupirire bodza; kuti aweruzidwe onse amene sanakhulupirira coonadi, komatu anakondwera ndi cosalungama. (2 Atesalonika 2:9-12)

KUPIRIZA KUPHUNZIRA

1. Zozizwitsa za Chipangano Chakale:

Werengani ma buku Eksodo ndi Deteronome. Unguzani zozizwitsa makumi awiri ndi zisanu zimene zinachitika mu nthawi ya Mose.

- Werengani ma buku 1 ndi 2 Mafumu. Tchulani zozizwitsa makumi awiri ndi chimodzi zimene zinachitika mu nthawi ya Eliya ndi Elisa.

2. Zozizwitsa za Chipangano Chatsopano:

- Werengani ma buku a Marko, Mateyu, Luka ndi Yohane ndipo tchulani zodabwitsa zimene Yesi anachitsa.
- Werengani buku la Machitidwe. Tchulani zodabwitsa zimene Mulungu anachita kudzera mwa atumwi ndi anthu ena amene anali kutimikira mu mpingo Oyamba.
- Werengani Machitidwe 9:36-41. Kodi ndi chozizwitsa chanji chimene chikuchitika apa? Kodi zotsatira za chozizwa chimenechi ndi chiani? (Machitidwe 9: 42)?
- Malingana ndi Aroma 15:18-19, Kodi ndi umboni wanji mu utumili wa Paulo umene unapangitsa kuti anthu amitundu amvere Mulungu?
- Werengani II Akorinto 12:11-12. Kodi ndi mphatso yanji yauzimu imene ikugwiriza ndi mphatso zozizwitsa?
- Kodi ndi zinthu ziti zimene zikuonetsera zozizwitsa ziti zimene zikuoneka pa Machitidwe 19:11-12?

MACHIRITSO

Koma kwa yense kwapatsidwa maonekedwe a Mzimu kuti apindule nao. Pakuti kwa mmodzi kwapatsidwa mphatso za maciritso, mwa Mzimu mmodziyo; (1 Akorinto 12:7-9 9).

Munthu amene ali ndi mphatso yamachiritso amakhala ndi kuthekera kolora mphamvu ya Mulungu kuti iyende ndikubweretsa machiritso. Machiritso amenewa amatchedwa machiritso a umulungu chifukwa chakuti amachokera kwa Mulungu osati kwa munthu.

Machiritso amene amephezeka m'baibulo anali apompopompo chifukwa chakuti anthu amachira pomwepo. Machiritso akuthupi ndi chizindiro chimodzi chimene chiyenera kutsata utumiki wa anthu onse okhulupirira.

Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; a; adzaika manja ao pa odwala, ndipo adzacira. (Marko 16:17-18)

wina aliyense amene ndi okhulupirira akhoza kupemphelera munthu odwala komanso akula ampango akhoza kupemphelera anthu odwala. Koma munthu amene ali ndi mphatso yamachiritso akhoza kugwiritsa ntchito mphatso yake mokhazikika pa utumiki.

Dzina la mphatso imeneyi limakonetsa kuti pali mphatso zosiyanasiyana za machiritso kapena kuti palinso njira zosiyanasiyana zakagwiritsidwe ntchito ka machiritso. Mulungu amatha kugwiritsa ntchito anthu ena kuti akachiritse nthenda zina zake. Mwachitsanzo, Baibulo limafotokoza kuti Mulungu anagwiritsa ntchito Paulo kuti akachite chozizwa chamachiritso (Machitidwe 19:11-12) Anthu ena okhulupirira amakhala ndi kuthekera kwapadera kopemphelera matenda apadera mwachitsanzo kupemphelera anthu akhungu. Pamene anthu ena ali ndi kudzodza kochiritsa matenda ena alionse.

Kupatura kuchiritsa matenda akuthupi, kuchotsa ziwanda ndi mizimu yonyansa ndi gawo limodzi la machiritso.

Komanso unasonkhana pamodzi unyinjira wa anthu ocokera ku midzi yozungulira Yerusalemu, alikutenga odwala, ndi obvutika ndi mizimu yonyansa; ndipo anaciritsidwa onsewa. (Macitidwe 5:16)

Chikhulupiriro ndi nsanamira yoti munthu alandire machiritso. Machiritso a Mulungu amatha kubwera kudzera muchikhulupiriro cha munthu amene akupemphelerayo. Yesu anaukitsa mtsikikana kwakufa ndi kumuchiritsa.

Koma pamene khamulo linaturutsidwa, Iye analowamo, nagwira dzanja lace; ndipo kabuthuko kadauka. (Mateyu 9:25)

Chifukwa chakuti mtsikanayu anali wakufa, kunali kosatheka kuti akhale ndi chikhulupiriro. Machiritso anabwelera kudzera mu chikhulupiriro cha Yesu Khristu.

Machiritso akhoza kubwera chifukwa cha chikhulupiriro cha munthu amene akudwala:

Koma Yesu potembenuka ndi kuona iye anati, Limba mtima, mwana wamkaziwe, cikhulupiriro cako cakuciritsa. Ndipo mkaziyo anacira kuyambira nthawi yomweyo. (Mateyu 9:22)

Machiritso amabweranso chifukwa cha chikhulupiriro cha munthu odwala ndi munthu amene akumpheleredwayo.

Ndipo m'mene Iye analowa m'nyumbamo, akhunguwo anadza kwa Iye; ndipo Yesu anati kwa iwo, Mukhulupirira kodi kuti ndikhoza kucita ici? Anena kwa Iye, Inde, Ambuye. Pomwepo anakhudza maso ao, nati, Cicitidwe kwa inu monga cikhulupiriro canu. (Mateyu 9:28-29)

Yesu anali ndi kuthekera kotha kuchiza munthuyu ndipo iye amadziwa kuthekera kwake. Koma izi pamodzi ndi chikhulupiriro cha munthu wakhungu uja zinabweretsa machiritso.

Pali njira zambiri zimene zimagwiritsidwa ntchito pofuna kuchita machiritso. Mwachitsanzo, machiritso amabwera chifukwa cha mau olankhuridwa ndi chikhulupiriro.

Koma kenturiyoyo anabvomera nati, Ambuye, sindiyenera kuti mukalowe pansu pa chindwi langa iai; koma mungonena mau, ndipo adzaciritsidwa mnyamata wanga. (Mateyu 8:8)

Atumiza mau ace nawaciritsa, Nawapulumutsa ku cionongeko cao. (Masalmo 107:20)

Machiritso amabweranso posanjika manja:

Ndipo pakulowa dzuwa anthu onse amene anali nao odwala ndi nthenda za mitundu mitundu, anadza nao kwa iye; ndipo iye anaika manja ace pa munthu ali yense wa iwo, nawaciritsa. (Luka 4:40)

adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzaika manja ao pa odwala, ndipo adzacira. (Marko 16:18)

Ndipo Mulungu anacita zamphamvu za pa zokha ndi manja a Paulo; (Macitidwe 19:11)

Machiritso amathanso kubwera kudzera mukudzodza mafuta mu dzina la Mulungu.

Pali wina kodi adwala mwa inu? Adziitanire akuru a Mpingo, ndipo apemphere pa iye, atamdzoza ndi mafuta m'dzina la Ambuye: ndipo pemphero la cikhulupiriro lidzapulumutsa wodwalayo, ndipo Ambuye adzamuukitsa; ndipo ngati adacita macimo adzakhululukidwa kwa iye. (Yakobo 5:14-15)

Machiritso anayambapo abwera kudzera muchithunzithunzi cha munthu amene ali ndi mphatso ya machiritso.

Ndipo unayankha mzimu woipa, nuti kwa iwo, Yesu ndimzindikira, ndi Paulo ndimdziwa, koma inu ndinu ayani? Ndipo munthu, mwa iye amene munali mzimu

woipa, anawalumphira nawaposa, nawalaka onse awiriwo, kotero kuti anathawa m'nyumba amarisece ndi olasidwa. (Macitidwe 19:15-16)

Tikhoza kukhala ndi machiritso chifukwa Yesu anazuzidwa ndi kutenga zowawa zathu zonse:

Koma Iye analasidwa cifukwa ca zolakwa zathu, natunduzidwa cifukwa ca mphulupulu zathu; cilango cotitengera ife mtendere cinamgwera Iye; ndipo ndi mikwingwirima yace ife taciritsidwa. (Yesaya 53:5)

Yesu anazuzidwa pamtanda paja osati kuti angotipulumutsa kumachimo athu okha ayi komanso ndi choling choti atipulumutse kunthenda zathu zonse. Iye anamenyedwa ndi kuzuzidwa ndi cholinga choti akachiritse nthenda zathu zonse komanso ndi cholinga choti tikapulumutsidwe.

Pamene tikupemphelera machiritso, tiyenera kuzindikira kuti si anthu onse amene angachire pamene tawapemphelera. Paulo akulankula za munthu wina amene sanachire ngakhale anapempheleredwa

Erasto anakhalira m'Korinto; koma Trofimo ndamsiya wodwala ku Mileto. (2 Timoteo 4:20)

Ngakhale kuti Paulo anali ndi mphatso yamachiritso, koma iye akufotokoza za munthu amene sanachire ngakhale kuti munthuyi anapempheleredwa. Paulo yemweyu anamulemberanso Timoteo pa zamatenda ake amgonagona:

Usakhalenso wakumwa madzi okha, komatu ucite naye vinyo pang'ono, cifukwa ca mimba yako ndi zofoka zako zobwera kawiri kawiri. (1 Timoteo 5:23)

Paulo sanasiye kugwirits ntchito mphatso yamachiritso chifukwa chakuti anthu ena amene anapempheleredwa sanachire ayi. Izi zili ngati mlaliki kusiya kulalika uthenga wabwino chifukwa chakuti anthu sanalandire uthenga atalalikidwa. Si munthu wina aliyense amene angalandira uthenga a Wabwino. Ngakhale kuti anthu ena amene anawapemphelera sanachiritsidwe, koma Paulo anapitilirabe kutumikira Mulungu. Iye analalikira ndi kupemphelera anthu odwala, koma zotsatira zazonsezi anazisiya mmanja mwa Mulungu.

Pali zifukwa zimene zimapangitsa kuti machiritso asabwere pamene munthu wapempheleredwa. Ndipo zifukwa izi ziperekedwa muphunziro lina la Harvstime Internnatioal la kufalisa Uthenga Wabwino.

POPITIRIZA KUPHUNZIRA

- Kutu muphunzire mwatsatanitsani zokhudza machiritso, pezani phunziro lina la Haverstime Internatioal lotchedwa “Nkhondo Yolimbanira Thupi”
- Werengani ma Buku a Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane kuti muone utumiki wa Yesu wamachiritso. Lembani mndandanda wamachiritso onse amene anachita ndipo lembaninso njira zimene iwo anagwiritsa ntchito.

- Werengani Buku la Machitidwe ndipo lembani mphatso zamachiritso zimene zimapezeka mu mpingo oyamba. Onetsetsani mitundu ndi njira zimene zimagwira ntchito pofuna kubweretsa machiritso.

Onani mu buku la Machitidwe anthu amene Mulungu anawagwiritsa ntchito ndi mphatso ya machiritso.

- Machitidwe 3:1-11: Petro ndi Yohane [apostles]
- Machitidwe 5:15; 9:32-34: Petro [mtumwi]
- Machitidwe 8:5-7: Filipo [Mlalili ndi mkulu wampingo]
- Machitidwe 9:17-18: Ananiya [samadziwika]
- Machitidwe 14:8-10; 28:7-9: Paulo [mtumwi]

Werengani ndime zili munsimuzi ndipo lembani zifukwa zimene Mulungu anapangira zozizwa: Yohane 9:1-3; Machitidwe 3:1-10; 4:4; Afili 2:25-27.

MALIRIME

Koma kwa yense kwapatsidwa maonekedwe a Mzimu kuti apindule nao. Pakuti kwa mmodzi kwapatsidwa; kwa wina malilime a mitundu mitundu; ndi kwa wina mamasulidwe a malilime (1 Akorinto 12:7-10)

Mphatso ya malirime ndikuthekera kolandira uthenga ochokera kwa Mulungu mu chilakhulo chimene sitimachidziwa kupita kwa anthu a Mulungu. Mau akuti malirime amatanthauza kuti chilankuro. Ndi zachidziwikire kuti Baibulo limafotokoza kuti malirime ndi chizindikiro kapena amaperekedwa ngati chizindikiro.

Pamene munthu wayankhula mumalirime, izi zikhoza kukhala chilankulo chimene anthu ena amachidziwa kapena chimene sangathe kuchizindikira.

Koma pocitika mau awa, unyinji wa anthu unasonkhana, nusokonezedwa, popeza yense anawamva alikulankhula m'cilankhulidwe cace ca iye yekha. Ndipo anadabwa onse, nazizwa, nanena, Taonani, awa onse alankhulawa sali Agalileya kodi? ndipo nanga ife timva bwanji, yense m'cilankhulidwe cathu cimene tinabadwa naco? (Macitidwe 2:6-8)

Komanso malirime akhoza kukhala chilankhuro chosadziwika ndi anthu ndipo izi zimatchedwa kulankhula mmalirime achilendo.

Pakuti iye wakulankhula lilime salankhula ndi anthu, koma ndi Mulungu; pakuti palibemunthu akumva; koma mumzimu alankhula zinsinsi. (1 Akorinto 14:2)

Monga mmene taonera kale kuti Kulankhula malirime ndi chizindiliro cha ubatizo wa Mzimu Woyera. Koma kulankhula malirime ngati chizindikiro cha ubatizo ndi zosiyana ndi mphatso ya Malirime. Mphatso ya malirime ndi kuthekera kwapadera kopereka uthenga wapadera kumpingo kudzera mu chilankhulo chimene olankhulayo samachidziwa.

Cholinga cha Malirime ngati chizindikiro cha ubatizo wa Mzimu Woyera komanso ngati mphatso ya Mzimu Woyera ndi ichi:

Kuti munthu apemphere kwa Mulungu: I Akorinto 14:2.

Kudzimangilira iwe mwini. I Akorinto 14:4 Kudzimangilira kumathandauza kudzilimbikitsa iwe mwini kapene kukula. Yesaya 28:11-12 imafotokoza izi ngati kutsitsimuka moyo wauzimu.

Kupembedzera: Mzimu Woyera amayankhula kwa munthu okhulupirira mumalirime ndi cholinga choti apembedzera pamene akupemphera. Mau oti kupembedzera amanthauza kupemphera mmalo mwa munthu wina. Mzimu Woyera amadziwa mmene tingapemphelere komanso chimene tiyenera kupemphelera. I Akorinto 14:21, Yesaya 28:11-13.

Matamando: Machitidwe 10:46, I Akorinto 14:15

Kukwaniritsa uneneri: I Akorinto 14:21; Yesaya 28:11-12

Mphatso ya malirime ili ndi zolinga ziwiri. Pamene munthu ali ndi mphatso ya malirime apereka uthenga wake ku mpingo, uthenga umeneu umayenera kumasuliridwa.

Kumangilira mpingo: I Akorinto 14:12-13

Ngati chizindikiro kwa anthu okhulupilira: Akorinto 14:22 Ichi ndi chifukwa chake mphatso ya malirime iyenera kuyenda limodzi ndi mphatso ya kumasilira malirime.

Pali ndondomeko zimene ziyenera kutsatidwa pamene mphatso Ya malirime ikugwiritsidwa ntchito mu mpingo.

1. Anthu onse asalankhule pakamodzi: I Akorinto 12:30
2. Ndi cholinga choti mpingo uthandizike, ndi zofunika kuti malirime ayenera kuyendera limodzi ndi mpato ya kumasulira malime ndi cholinga choti anthu amve zimene zikukambidwa.
3. Chifukwa cha ichi, munthu amene ali ndi mphatso ya malirime ayenera kukhala chete ngati palibe munthu oti amasulire: I Akorinto 14:18-19.
4. Munthuyo ayera kupemphelera mphatso yomasulira malirime. I Akorinto 12:13
5. Ngati mumpingo mulibe munthu amene akhoza kumasulira malirime, ndi bwino kuti mulankhure muchilankhulo chimene anthu akhoza kumvetsa.
6. Munthu mmodzi ayenera kumasulira pakamodzi: I Akorinto 14:27.
7. Munthu amene ali ndi mphatso ya malirime ali ndi udindo pa mphatso yake. I Akorinto 14:32-33
8. Anthu sayenera kuletsedwa kulankhula malirime I Akorinto 14:39-40.
9. Chinthu chofunika kwambiri ndi chakuti payenera kukhala dongolo mu mpingo. Pasakhale chisokonezo chobwera chifukwa cha mphatso za Mzimu Woyera I Akorinto 14:40.

POPITIRIZA KUPHUNZIRA

- Werengani 1 Akorinto 12-14 ma chaputala awa amatsindika kagwiritsidwe ntchito ka mphatso zauzimu makamaka mphatso ya malirime komanso mphatso ya mamasuridwe a a malirime pa chaputala 14.
- Werengani zolinga za mphatso zimenezi zikupezeka pa 1 Akorinto 14:4,5,22.
- Kodi ndi ndondomeko zANJI zimene zinakhazikitsidwa pakagwiritsidwe ka ntchito ka mphatso pamene anthu akumana mu mpingo? Werengani 1 Akorinto 14:26-28.
- Mphatso ya malirime ndi chizindikiro kwa anthu osakhulupirira. Malingana ndi ndime zili munsimuzi, tchulani anthu amene anali osakhulupirira ndi kumene amachokera

	Anali ndani.	Machokera kuti
- Machitidwe 2:2-13	_____	_____
- Machitidwe 10:24 -28	_____	_____
- Machitidwe 19:1-7	_____	_____

KUMASULIRA MALIRIME

Koma kwa yense kwapatsidwa maonekedwe a Mzimu kuti apindule nao.; ndi kwa wina mamasulidwe a malilime. (1 Akorinto 12:7-10)

Mphatso yakumasulira malirime ndi kuthekera kwapadera kotha kumasilira malirime osamveka kuti amveke muchilankhuro chomveka kwa anthu. Kumasulira malirime kumaperekedwa ndi Mzimu Woyera kwa munthu amene walandira mphatsoyi. Siziri ngati kumasulira chilankhulo chimene munthu amachidziwa kale. Izi zimatheka kudzera mu mavumbulutso a Mzimu Oyera. Kumasira malirime kumakhala ngati kufotokozerwa mwachidule zinthu zimene zalembedwa osati kumasulira mau ena alionse amene anenedwa.

Cholinga cha mphatso ya kumasulira malirime osamveka:

Cifukwa cace wolankhula lilime, apemphere kuti amasule. Koma ngati palibe womasulira, akhale cete mu Mpingo, koma alankhule ndi iye yekha, ndi Mulungu. (1 Akorinto 14:13,28)

Munthu amene ali ndi mphatso ya malirime ayenera kupemphelera mphatso ya kumasulira malirime:

Cifukwa cace wolankhula lilime, apemphere kuti amasule. (1 Akorinto 14:13)

POPIRIZA KUPHUNZIRA:

- Werengani 1 Akorinto 14 kuti mupeza ndondomeko za kwagwiritsidwe ntchito ka mphatso za mamasiridwe a malirime.
- Kodi zotsatira za malirime pemene amasuliridwa ndi chiani? Werengani 1 Akorinto 14:5.

- Kodi chimayenera kuchitika ndi chiani pamene palibe munthu oti amasulire malirime (werengani 1 Akorinto 14:28)
- Kodi amayenera Kumasulira malirime ndi ndani (14:13 ndi 27).
- Kodi ndi nyengo iti imene mphatso yamalirime sikuyenera kugwiritsidwa ntchito.

KACHITIDWE KA UTUMIKI WA MPHAMVU

Chaputala ichi ndi chomariza pa nkhani ya mphatsi za Mzimu Woyera. Ndipo taona kuti mphatso zimenezi zagawidwa mmagawa angapo amene ndi awa:

- Mphatso zapadera
- Mphatso zakutumikira
- Zindikiro za mphatso
- Mphatso zolankhula

Chithunzi chili pansichi chikuonetsa magawo amphatso izi komanso mmene zimagwilira ntchito mumpingo kuti utumiki uyende bwino.

MPHATSO ZAPADERA

- Mtumwi
- Mneneri \Rightarrow KUKONZEKERETSA ANTHU A MULUNGU
- Mlariki
- M'busa
- Mphunzitsi

MPHATSO ZOLANKHULA

KUFOTOKOZERA CHOONADI CHA MULUNGU \Rightarrow Uneneri

- Kuphunzitsa
- Kudandaulira
- Mau a mzeru
- Mau a chidziwitso

MPHATSO ZOTUMIKIRA

- KUTUMIKIRA
- Kuthandizira
- Kuyendetsa zinthu \Rightarrow KUTHANDIZIRA NTCHITO YA MULUNGU
- Kupereka
- Kuonetsa chifundo
- Kuzindikira mizimu
- Chikhulupiriro
- Kuchereza alendo

ZIZINDIKIRO ZA MPHATSO

KUKHAZIKITSA ULAMULIRO \Rightarrow

Malirime
Kumasulira
Zozizwitsa
Machiritso

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

2. Kodi zizindikiro zinayi za mphatso ndi ziti?

3. Malingana ndi Yohane 20:30-31, kodi zolinga ziwiri za mphatso ya zozizwa ndi chiani?

4. Onani zizindikiro za mphatso mu mndanda oyamba ndipo werengani tanthauzo limene likupezeka mu mdandanda wachiri. Lembani nambala imene ikufotokoza tanthauzo la mphatso pa mpata umene waperekedwa.

Mndandanda oyamba

____Machiritso

____Malirime

____kumasulira

____zozizwitsa

mndandanda wachiwiri

1. Zochitika zamphamvu zimene sizingachitike pazokha kapena mwachilengedwe.

2. Mphamvu ya Mulunguyobwenzeretsa thanzi posagwiritsa ntchito njira zakuthupi

3. Kulankhula chilankhulo chachilendo kwa munthu olankhulurayo

4. Kumasulira uthenga wamalirime ndi cholinga kuti umveke

5. Werengani ziganizo zili munsimuzi. Ngati chiganizo chili cholondora, lembani T kutsogolo kwachiganizocho ndipo ngati chiganizo sichiri cholondora lembani F kutsogolo kwachiganizo.

a. ____kulankhula malirime ngati chizindikiro cha ubatizo wa Mzimu ndi chimodzimodzi ndi mphatso ya Malirime

b. ____munthu amane ali ndi mphatso ya malilime akhale chete mumpingo ngati palibe munthu oti amasulire

c. ____ Munthu amene ali ndi mphatso ya malilime akuyenera kumasulira uthenga wake omwe.

d. ____ Munthu amene ali ndi mphatso yamalirime sangathe kuchitapo kathu pakagwiritsidwe

ntchito ka Mphatso yake;

- e. ___ Ndibwino kulankhula muchilankhulo chimene anthu mu mpingo amaamva kusiyana ndi
ndi kulankhula malirime popanda kutanthauzira
- f. ___Anthu angapo akhoza kutanthauzira uthenga umodzi pa nthawi imodzi
- g. ___ Ngati munthu ali ndi mphatso yamachiritso, munthu wina aliyense amene
angampemphelere ayenera kuchiritsidwa.
- h. ___Munthu yekhaya amene ali ndi mphatso yamachiritso ayenera kupemphelera odwala.

(mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA.

Zoonjera zina zinakambidwa kale ndi cholinga choti muthe kumaliza maphunziro anu okhudza mphatso ina iliyonse payokhapayokha. Koma mu gawo uli tiona mmene mphatso zonsezi zimaonekera mu utumiki wa Yesu Khristu.

MPHATSO ZA MZIMU WOYERA MMOYO WA YESU KHRISTU

-zozizwitsa:	Machitidwe 2:22
-Machiritso:	Machitidwe 10:38
-Mau a Mzeru:	I Akorinto 1:24,30
-Mau a Chidziwitso:	Yohane 1:45-50; 4:18; 11:14
-Kuzindikira Mizimu:	Yohane 1:45-50 6:61
-Uneneri /Mneneri	Mateyu 24
-Kuphunzitsa /mphunzitsi:	Mateyu 4:23; 9:35; 26:55; Marko 6:6; 14:49; Luka 5:17; 13:10,22; 21:37
-Kudandaulira:	Luka 3:18
-Chifundo [Kukhudzika]:	Matetuyu 20:30-34
-Mtumwi:	Ahebrew 3:1
-Mlariki:	Yohane 10:16
-M'busa:	Yohane 10:11
-Utsogoleri:	Yohane 13:15-16; Marko 10:42-45
-Kuyendetsa zinthu:	Luka 10:1-17
-chikhulupiriro:	Luka 8:49-56
-Kupereka:	Yohane 10:11
-Kuthandizira:	Yohane 17:6-10
-Kutumikira:	Yohane 13:4-16; Marko 10:42-45
-Kuchereza alendo	Yohane 21:9-13 [Alibe khomo koma amachereza alendo].:

Malirime ndi kumasulira: Izi zinali mphatso ziwiri zimene sizinaonekera mmoyo wa Yesu Khristu. Izi sizinali zofunikira chifukwa chakuti iye anali Mau a Mulungu. Panalibe kufunika koti alandire mau a Mulungu kuchokera kwa Mulungu kudzera mwa munthu.

CHAPUTALA 10

KUZINDIKIRA MPHATSO YANU YAUZIMU

ZOLINGA:

Pamapeto pa chaputala ichi muyenera kudziwa zinthu izi:

- Kufotokozero kufunika kozindikira mphatso zauzimu kwa okhulupirira.
- Kufotokozero mmene okhulupirira angazindikire mphatso zao zauzimu.
- Kuzindikira mphatso yauzimu

VESI YOTSOGOLERA:

Cifukwa cace ndikukumbutsa iwe ukoleze mphatso ya Mulungu, iri mwa iwe mwa kuika kwa manja anga, (2 Timoteo 1:6)

MAU OYAMBA

Chaputala chapitachi, tinaona kuti okhulupirira wina aliyense amakhala ndi mphatso imodzo yauzimu.

KUFUNIKA KOZINDIKIRA MPHATSO YAUZIMU

Ndi zofunika kuzindikira mphatso yauzimu pa zifukwa izi:

KUTI MUKWANIRITSE ZOLINGA ZAUZIMU:

Kumbukirani zolinga za mphatso za Mzimu Woyera zimene zaperekedwa pa Aefeso 4:12-15.

- Kuti mukhale angwiro.
kupititsa patsogoro ntchito yautumiki
- Kuthandiza Khristu ndi mpingo.

Zofuna kukwaniritsa:

- Timakhala paumodzi muchikhulupiriro.
- Tikuze chidziwitso chathu cha Khristu
- Timakulebe mu ungwiro poyang'anira khristu ngati chifaniziro chathu.
- Timakhazikike, osanyengeka ndi ziphunzitsa zonyenga.
- Tikule mwakhristu moyo wathu wauzimu.

Kuti zolinga zimenezi zikwaniritsidwe ndi zofunikwa kuti okhulupirira wina aliyense ayenera kuzindikira mphatso zauzimu komanso kutha kudziwa magwiritsidwe ntchito a mphatso zimenezi.

KUTI MUKAMENYE NKHONDO YAUZIMU

Mphatso zauzimu zimaperekedwa ku mpingo ngati zida zomenyenyerera nkondo yolimbana ndi asirikari a Satana.

Cifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba. (Aefeso 6:12)

Ndi zofunika kutha kuzindikira ndi kugwiritsa ntchito mphatso zanu zauzimu kuti mukathe kumenya nkondo yolongosoka yolimbana ndo mdani wanu amene ali Satana.

KUTI MUPEWE KUGWIRITSA NTCHITO MOLAKWIKWA MPHATSO ZIMENEZI

Mu chaputala cha mbuyomu, taona njira zitatu zakagwiritsidwe ntchito kolakwika ka mphatso zauzimu:

1. Posagwiritsa ntchito mphatso zimene Muli nazo.
2. Kuyesera kugwiritsa ntchito mphatso zimene inuyo mulibe.
3. Kugwiritsa ntchito mphatso zanu mosayenera.

Ndi zofunika kuzindikira mphatso zanu zauzimu ndi cholinga choti mupewe kugwiritsa ntchito mphatso zanu molakwika.

KUTI MUPEWE KUGWA MPHAYI:

Okhulupirira ambiri amayamba utumiki asayambe azindikira mphatso zao. Chifukwa cha ichi, amakhala ofooketsedwa kapena akugwa mphwayi ngakhale ogonjetsedwa kumene pamene ayamba kuchita utumiki. Nanunso mukhoza kukhumudwitsidwa ngati zimuzindikira mphatso zanu zauzimu. Simungatumikire mwampamvu ngati mungatumikire mu utumiki umene Mulungu sanakupatseni ngati mphatso yanu.

Mukhoza kukangalika muutumiki, koma palibe chimene mungakwaniritse ku Ufumu wa Mulungu. Mwachitsanzo, munthu wina ayenesa kutengera mmene mtumiki Billy Graham amachitira. Iye anafika pomalalika ngati Billy Graham, koma palibe ndi mmodzi yemwe amene anasunthika ndi uthenga wake. Iye anali okhumudwa ndi utumiki wake kufikira nthawi imene anzindikira kuti mphatso yake sinali kulalika koma kuphunzitsa. Iye atayamba kugwiritsa ntchito mphatso yake yauphunzitsi, zotsatira zake zinayamba kuonekera.

Kuzindikira mphatso zanu kumathandiza kuti mupewe kukhumudwa nokha, komanso izi zimathandiza kuti musakhale okhumudwa ndi anthu ena okhulupirira. Mwachitsanzo, mukhoza kuzindikiridwa ngati m'busa wabwino koma osadziwa kuyendetsa zinthu. Mukhoza kuzindikira kuti m'busa wanu ali ndi mphatso yauphunzitsi osati yakayendetsedwe kazinthu kapena yautsogoleri. M'malo moyamba kumudzudzula, choyenera kuchita ndikupeza thandizo la munthu amene ali ndi mphatso imene alibe kuti mpingo uyende bwino.

KUTI MUKATENGE UDINDO WANU:

Mukuyendera kuzindikira mpatso yanu chifukwa muli ndi udindo ogwiritsa ntchito mpatso yanu. Mtumwi Paulo anafotokoza:

Usanyalapse mpatsoyo iri mwa iwe, yopatsidwa kwa iwe mwa cinenero, pamodzi ndi kuika kwa manja a akulu... (1 Timoteo 4:14)

Cifukwa cace ndikukumbutsa iwe ukoleze mpatso ya Mulungu, iri mwa iwe mwa kuika kwa manja anga, (II Timoteo 1:6)

Muyenera kuzindikira mpatso yanu ndi cholinga choti mukwaniritse udindo wanu okuza mpatsoyo. Ndikoyenera kudziwa mpatso yanu ndi cholinga choti muthe kuchita zinthu zoyenera kuti mpatsoyo ikagwire ntchito moyenera.

KUZINDIKIRA MPHATSO YANU

Ndondomeko izi zikhoza kukuthandizani kuti muzindikire mpatso zanu zauzimu:

NJIRA YOYAMBA- kubadwa mwatsona.

Muyenera kubadwa mwatsopano. Mpatso zauzimu zimabwera pamene munthu wabadwa mwatsona ngati chimodzimodzi mmene munthu amwabadwira ndi luso. Ngati munthu sanabadwe dziku lakuthupi, ndi zosatheka kukhala ndi luso. Komanso ngati munthu sangabadwe mwatsopano mudziko lauzimu, munthu amaneyu sangalandire mpatso yauzimu.

Koma Petro anati kwa iwo, Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku cikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mpatso ya Mzimu Woyera. (Macitidwe 2:38)

NJIRA YACHIWIRI: Kulandira ubatizo wa Mzimu Woyera.

Ndondomeko zimene mungalandilire ubatizo wa Mzimu Woyera zaperekedwa mu chaputala 4.

NJIRA 3 – kuzindikira mpatso zauzimu

Ngati simumadziwa mpatso zauzimu, simungazindikire mpatso imene Mulungu anakupatsani. Phunziro limene mwaphunzira mu maphunziro awa likuthandizani kuti muzindikire mpatso zimene okhulupirira akhoza kukhala nazo.

NJIRA 4 Kuyang'anira anthu ena amene ali ndi mpatso zimene mumasilira:

Pamene mukusinkhasinkha mpatso imene Mulungu anakupatsani, ndi zofunika kuti muyang'anire anthu amene ali ndi mpatso imene muli nayo. Chitsanzo chabwino cha munthu amene mungathe kumutenga ngati chitsanzo chanu ayenera kukhala okhulupirira okhwima komanso amene wakhala akugwiritsa ntchito mpatso yake kwa nthawi yaitali.

Mwachitsanzo, mukhoza kucheza ndi munthu amene ali ndi mpatso ya uphunzitsi. Afunseni kuti anadziwa bwanji kuti ali ndi mpatso, mmene anayambira kuigwiritsa ntchito, njira zimene akugwiritsa ntchito kuti akuze mpatso yawoyo. Kuphunzira kuchokera kwa anthu ena mmene

anazindikira mphatso yawo komanso kukhala ndi zitsanzo zabwino za anthu amene ali ndi mphatso zauzimu zikhoza kukuthandizani kuti nanunso muzindikire mphatso zanu.

Njira 5- funafunani mphatso yauzimu.

Muyenera kukhumba mphatso yauzimu ndi kuyisalira chakudya. Baibulo limafotokoza kuti tikuyenera kukhumbitsa mphatso yauzimu.

**Koma funitsitsani mphatso zoposa. Ndipo ndikuonetsani njira yokoma yoposatu.
(1 Akorinto 12:31)**

Wina aliyense ali ndi mphatso imodzi, koma vesi imeneyi ikutanthauza kuti tikhoza kufunafuna mphatso imene tilibe.

NJIRA 6- Kusanjikidwa manja:

Kodi atsogoleri anu auzimu anayamba akusanjikanipo manja ndi kukupemphelerani:

**Koma funitsitsani mphatso zoposa. Ndipo ndikuonetsani njira yokoma yoposatu.
(1 Akorinto 12:31)**

Potsata njira 1 mpaka njira 6, Mulungu ankhoza kukuvumbulutsirani mphatso yanu. Koma ngati sizinachitike, muyenera kupirizabe ndi njira zili munsizi.

NJIRA 7- unikirani zinthu zimene mumakonda:

Ma gawo amene mumakhala nawo omasuka mukatumikira ndi amene amakhala kuti ndi amene Mulungu anakupatsani ngati mphatso yanu. Mphatso imene munthu amalandiira kuthupi uimabweretsa chimwemwe chomwechonso, mphatso yauzimu imabweretsa chimwemwe. Muyenera kukhala ndi chilakolako kapena chikhumbokhumbo chachikulu kuti mutumikire Mulungu moyenera.

Mwachitsanzo, munthu amene ali ndi mphatso yautsogoleri akhoza kugwiritsa mphatsoyi poyendetsa chinachililichonse. Akhoza kuyendetsa zinthu ngati masukulu a chikhristu ndi zinthu zambiri. Koma chofunika ndi chakuti munthuyo ayenera kukhala ndi chikhumbokhumbo chachichikulu chofuna kutumikira. Munthuyo ngati alibe chidwi choyendetsa sukulu ya chikhristu sangakhalitse posatengera kuti ali ndi mphatso ya utsogoleri.

Yankhani mafunso awa kuti akuthandizeni kuzindikira pamene pali chidwi chanu.

1. Kodi ndi gulu liti la anthu limene mumakopeka nalo mtima?

(ngati munaitanidwa kuti mukatumikire ku gulu la anthu ena ake, mphatso zanu zimakhala zogwirizana ndi zosowa zao. Ngati mukumva kuitanidwa kuti muchite utumiki wa ana, mukhoza kukhala ndi mphatso yachiphunzitsa.)

2. Kodi ndi magawo ati amene pali zosowa zimene mumakhudzika nazo.

(Ngati Mulungu wakuitanani kuti mukumane ndi chosowa chinachake, mumamva kukakamizika mkati mwanu)

3. Kodi mutakhala kuti mwalephera ndi chiani chimene mungakhumbe kuti muchitire Mulungu.

(Mulungu amalemekeza zimene timakhumba)

4. Malizitsani chiganizo ichi, “ndili kutsikimizika mtima kwakukulu kuti ndi chitepo kanthu, kodi ndichite chiani...”

Nthawi zambiri kukhala ndi kutsikimizika kwakukulu zimakhala kuti Mulungu akulankhula ndi mzimu wanu pa zimene iye akufuna kuti inuyo mutumikire.

5. Ndili ndi kutsikimizika mtima kuti Mulunguwanditanira ku utumiki wa ...

Ngati mukutha kuzindikira utumiki umene Mulungu anakuitanirani, zimakhala zosavuta kudziwa mphatso yauzimu imene muli nayo. Mulungu amapereka mphatso ndi cholinga choti mukwaniritse Maitanidwe. Gawo la maphunziro owonjezera likuthandizani kuti muzindikire maitanidwe anu.

6. Kodi ndi mphatso ziti zimene zimabweretsa chimwemwe pamene mwazigwiritsa ntchito. (mwachitsanzo, kodi mumakondweretsedwa ndi kuphunzitsa? kapena mumakonda kulandira alendo pakhomo panu? Kapena mumasunthika ndi kupereke ndalama zochuluka kwambiri ku ntchito ya Mulungu?)

NJIRA 8- Mtsogoleri wachikhristu awunikire mphatso zanu:

Muyenera kupeza mtsogoleri wachikhristu kuti awunikire kuthekera kwanu. Muyenera kufunsa mafunso awa ndipo lembani mayankho amafunsowo.

1. Kodi ndi magawo ati autumiki amene mukuona kuti ndimachita bwino.

-
2. Malingana ndi zinthu zimene ndimachita bwino, kodi ndi mphatso ziti zimene mukuona kuti ndili nazo?

NJIRA 9- unguzani zinthu utumiki wanu wakale

Miyenera kuunikira utumiki wanu wakale. Yankhani mafunso awa.

1. Kodi ndi magawo ati a utumiki wachikkhristu amene mwakhala mukutumikira mbuyomu?

2. Kodi ndi magawo ati amene munachita bwino?
3. Kodi ndi gawo liti limene linabweretsa chimwemwe chachikulu pamene mumatumikira?

4. Kodi ndi magawo ati amene atsogoleri anu kapena anthu ena anawona kuti munachita bwino?

NJIRA 10- Malizitsaniz kuysankha mafunso awa:

Gawo lomaliza la phunziro ili liri ndi mafunso okhudza mphatso zauzimu. Mayankho anu kumafunso amenewa akuthandizani kuti muzindikire mphatso zimene muli nazo.

Zindikirani mphatso zimene mukuona kuti muli nazo pogwiritsa ntchito zinthu izi:

1. Pogwiritsa ntchito chidziwitsop cha mphatso zauzimu chimene mwachipeza kudzera mu phunziro ili.
2. Zimene Mulungu wakuonetserani kudzera mu pemphero.
3. Zimene mwatha nokha kuzindikira.
4. Zimene atsogoleri achikhristu aziona mwa inu.
5. Kuunikira magawo a utumiki amene munachita bwino mbuyomu.
6. Kugwiritsa ntchito mafunso okhudza mphatso zauzimu

Ndandanda wa mphatso zauzimu waperekedwa munsimu. Choyenera kuchita ndi kuika X pamene pali mphatso imene mukuona kuti muli nayo.

NJIRA 12- zindikira zosowa zauzimu:

Pounikira zosowa zauzimu za dera lanu, anthu amene mumakhala nao komanso zosowa zokhudza mpingo wanu. Wonani mndandanda wa zinthu zosowa zili munsizi:

Kuyendera anthu: odwala, oyamba kumene mpingo, zipatala, azimayi amasiye, andende, oferedwa, komanso okalamba.

Kufalitsa uthenga: kuyenda khomo ndi khomo, kudzera mmisonkhano, pabwalo la anthu ambiri.

Kulimbikitsa: Anthu ongotembenuka mtima kumene.

UPHUNGU: kupereka uphungu kwa anthu osiyanasiyana ngakhale pogwiritsa ntchito zinthu ngati foni.

KUYENDE TSA ZINTHU KAPENA KUTHANDIZIRA: kulemba zinthu, kulemba makalata ndi zinthu zolembedwa.

Kuchereza alendo: kuphikira ndi kupereka malo ogona kwa atumiki ongobwera kudzatumikira.

UTUMIKI KWA OSAUKA: Kupereka chakudya, dzovala ndi malo okhala kwa anthu ovutika.

KUKONZA NYUMBA YOPEMPHELERAMO: kupaka penti, kukhoma zinthu zofunika kukhoma, kusesa ndi kukolopa ndi zina zambiri.

MAIMBIDWE: kwaya, kusewera dzida, magulu anyimbo, kapena kulemba nyimbo kumene.

Kuchita zisudzo zauzimu. Kulemba zisudzo zauzimu.

Zokhudza ndalama: kupeza njira zopezera ndalama, kuwerengetsera ndalama komanso kuchita ndongosolo la kagwiritsidwe ntchito ka ndalama.

Kulemba: kulemba mabuku achikhristu, nyuzi pepala ndi zina zambiri.

Utumiki kwa anthu a ulumari: anthu akhungu, amisala, oledzera mwa uchidakwa, ochita zinthu zogonana amuna kapena akazi okhaokha.

Maudindo a mumpingo: mkulu wampingo, mphunzitsi wa ana, othandizira chipembedzo kapena oyendetsa ntchito zosiyanasiyana monga zomangamanga.

Maphunziro achikhristu: maphunziro a ana, maphunziro a Baibulo, sukulu ya ana ang'ono, masukulu a ukachenjede, kuphunzitsa anthu wamba mu mpingo pogwiritsa ntchito maphunziro a Haverstime International Institute.

Kudzala mipingo kapena utumwi: kufikira anthu amene sanafikikilidwe ndi uthenga wabwino kwa anthu a mdziko lanu kapena maiko ena.

Zolembalemba: nyumba zosungilira mabuku achikhristu, ma Baibulo ndi zolembedwa zina zokhudza Baibulo.

Tsopano yakhani mafunso awa:

1. Kodi ndi zosowa ziti zimene sizikufikiridwa kumene mumakhala.

2. Kodi ndi zinthu ziti zimene sizikufikiridwa mu dera lanu.

3. Kodi ndi zosowa ziti zimene zikufikiridwa mu mpingo wanu?

Njira 13- Kwaniritsani chosowa chauzimu:

Zinthu zimene mwaphunzirazi zikhoza kukhala zopanda kanthu ngati simungathe kuzigwiritsa ntchito mmoyo wanu kapena pa utumiki. Izi zikutanthauza kuti muyenera kugwiritsa ntchito mphatso yanu moyenelera kuti muchite kenakake.

Fanananizana mdandanda wa mphatso zimene zikupezeka pa Njira ndi mdandanda wa mphatso zimene mukuona kuti Mulungu anakupatsani. Pezani zosowa zauzimu zimene zikugwirizana ndi mphatso zanu ndipo kwaniritsani zosowa zimenezi mudera limene mumakhala, mwachitsanzo ngati mukuona kuti pali kusowelera kwa aphunzitsi mu mpingo mwanu ndipo inuyo muli ndi mphatso yauphunzitsi dziperekeni nokha kuti mukwaniritse mphatso imeneyi. Ngiwiritsani ntchito zinthu zalembedwa pansipa:

Kulumukiza chosowa chauzimu ndi mphatso

Ndikukhulupirira kuti ndiri ndi mphatso izi. Mphatsoyi ikhoza kukumana ndi zosowa za Mdera, mumpingo anthu okhala nao pafupi

___ Mtumwi _____
___ Mneneri _____
___ Mlaliki _____
___ M'busa _____
___ mphunzitsi _____
___ kulimbikitsa _____
___ mau a luntha _____
___ Mau a chidziwitso _____
___ Kutumikira _____

Ndikukhulupirira kuti **Mphatso imeneyi ikhoza kukumana ndi zosowa mu**
ndili ndi mphatso izi

___ Kuthandiza _____
___ Utsogoleri _____
___ Kuyendetsa zinthu _____
___ Kupereka _____

___ kuonetse chifundo _____

___ Chidziwitso cha Mizimu _____

___ chichikhulupiriro _____

___ Kuchereza alendo _____

___ Malilime _____

___ kumasulira malilime _____

___ Zozizwitsa _____

___ Machiritso _____

NJIRA 14- Unikirani Jutumiki Wanu:

Mutatumikira kwa kanthawi pogwiritsa ntchito mphatso yanu, muyenera kuunikira utumiki wanu. Kodi mukutha kuona kuti mukugwiritsa ntchito bwino mphatso yanu yauazimu.

- Ngati mukubala zipatso mdera limene mukutumikira, izi zimatanthauza kuti zotsatira za utumiki wanu zimakhala zabwino.
- Ngati mukukwaniritsidwa ndiye kuti mukukondwera ndi utumiki wanu. Ngati mukumakhala okhumudwa ndiye kuti mukutumikira dera limene si gawo lanu.
- Ngati ndemanga zimene atsogoleri amakamba zimaonetsa kuti mukuchita bwino.

Ngati utumiki umene mukuchita siukugwirizana ndi kuthekera kwanu kapena mphatso zanu, simungathe kuchita bwino. Choyenera kuchita ndi kuunikira mphatso zina ndikupempha Mulungu kuti akuonetsera gawo lina loti mutumikire.

Simukuyenera kubwelera m'mbuyo Kumbukiran nkhanu ya munthu uja amene amkaona ngati ndi mlaliki koma chonsecho iye anali mphunzitsi. Ndi zofunika kuzindikira mphatso zimene mulibe ndi cholinga choti muzindikire mphatso yanu. Izi zimakuthandizani kuti mupewe kutaya nthawi yanu pa utumiki umene simungakhale ndi mphindu lochuluka. Pogwiritsa ntchito pemphero ndi njira zimene zafotokozeredwa mu buku limeneli zikhoza kukuthandizani kuti mukazindikire mphatso yanu yautumiki. Ndipo pamene mwayamba kutumikira, mudzazindikira mpatsao yanu yautumiki.

MAYESO ODZIYESA NOKHA.

1. Lembani vesi yotsogolera

2. Tchulani zifukwa zisanu zakufunika kozindikira mphatso yanu?

3. Tchulani njira khumi ndi zinayi zimene zingathandize kuti muzindikire mphatso yanu

(mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa phunziro ili)

ZOONJERA POPHUNZIRA

1. Mulungu nthawi zonse amapereka mphatso zoti zikuthandizeni kukwaniritsa maitanidwe anu auzimu. Kodi mungadziwe bwanji kuti munaitanidwa. Werengani chifaniziro cha kuitanidwa kwa Mose:

Mulungu amapereka chitsogozo:

Werengani Eksodo 3:1-4. Mfundo yoyamba yakuzindilira kuti Mulungu ndi amene amaitana munthu. Iye ali ndi udindo olumikizana ndi munthu pa zimene akufuna kulankhula kwa munthuyo.

Simukuyenera kuyamba kuunguzaunguza muli okhumudwa pa chimene Mulungu akufuna kuti inuyo muchite. Sikoyenera kuti mukhale mukufunsa anthu maganizo awo pa zinthu zimene mukufuna kuti muchite. Ndi udindo wa Mulungu okha kuti alankhule zimene iye akufuna kuti muchite ngati maitandwe anu. Maitanidwe enieni a Mulungu si chinthu chimene mumachita nokha kusankha kuti muchite kapena zimene anthu ena akuganiza kuti muyera kuchita.

Mumakhala ndi njala yaikulu.

Kwa dzaka zambiri, Mose anali ndi njala mkati mwake pa anthu ake, ana a Israeli. Iye anali otsikimikizika kwambiri ndi izi kufikira kuti anapha munthu waku Aigupto (Eksodo 2:11-15). Pamene Mulungu wakuitana ku utumiki wina wake wapadera, mumamva njara mkati mwanu, kapena kuti mumakhala ndi chidwi ndi kukhudzika kwakulu.

Mumalandira Dongosolo Lochokera Kwa Mulungu:

Kukhala ndi njala mkati mwanu, kukhudzika kapena kukhal ndi chidwi chachikulu si zizindikiro zokwana kuti mukwaniritse maitanidwe anu. Kuonjezera zimenezi, Mulungu amalankhula chifuniro chake ndi cholinga choti mukwaniritse maitanidwe anu.

Apa ndi pamene anthu ambiri amalephera. Amalandira maitanidwe kuchokera kwa Mulungu koma amathamangira kufuna kukwaniritsa maitanidwe aja osanadikire Mulungu kuti awonetsera dongosolo lake.

Mulungu anapereka dongosolo lonse kwa Mose. Iye ndi Aroni amayenera kuti akafike pamaso pa Farao ndi kumuusa kuti amasure ana a Israeli. Iwo amayenera kutsogolera anthu muchipululu kufikira mudziko lamalonjezano. Pamene Mulunguwakupatsana maitanidwe, muyenera kudikira kufikira nthawi imene mwalandira dongosolo lonse lokhudza maitanidwe anu.

Mumamva kupelewera mkati mwanu:

Pa Eksodo 3: 8, timaona zakuperewera kwa Mose, Iye anati “ine ndi yani kuti ndikafike pamaso pa Farao ndikukaturutsa ana a Israeli mwa Igupto”

Pamene mwalandira maitanidwe enieni ochokera Kwa Mulungu, nthawi zonse mumamva kupelewera. Ngati mumamva chikwanekwane mkati mwanu, muyenera kukhala osamala chifukwa zikhoza kukhala kuti izi sizochokera kwa Mulungu. Pamene Mulungu wakuitanani, mumamva kuperewera. Mumaona ngati inuyo ndi munthu osayenera kuti mukakwanirise zimene

Mulungu wakuitanirani kuti muchite, ndipo mumkhala odabwitsidwa ndi ntchito imene Mulungu wakupatsani.

Werengani nkhani za anthu ena mu Baibulo ndipo muzindikira kuti maitanidwe awo ndi Mulungu anali ofanana. Mwachitsanzo, werengani zakuitanidwa kwa Gideoni mu Buku la Oweruza 6 komanso za kuitanidwa kwa Yereimiya pa Yereimiya 1.

Mdandanda uli munsimu ukuthanthandizani kuti kuti mudziwitsitse njira zothandiza kuzindikira mphatso yanu zauzimu.

Njira 1 ____ Ndinabadwa mwatsopano.

Njira2 ____ Ndinalandira ubatizo wa Mzimu Woyera.

Njira 3 ____ Nditha kuzindikira mphatso zosiyanasiyana zauzimu.

Njira 4 ____ Ndaonenera zitsanzo zabwino za mphatso zauzimu.

Njira 5 ____ Ndafunafuna mphatso zauzimu kudzera mupemphero ndi kusala kudya

Njira 6 ____ Ndinasanjikidwa manja ndi atsogoleri anga auzimu ndikupemph Mulungu aonetsera mphatso zanga

Njira 7 ____ Ndaunikira zokonda zanga zauzimu.

Njira 8 ____ Ndaunikira atsogoleri anga auzimu.

Njira 9 ____ Ndaunikira utumiki wanga wakale wachikhristu.

Njira 10 ____ Ndamaliza kuyankha mafunso okhudza mphatso zauzimu.

Njira11 ____ Ndazindikira mphatso zauzimu zimene ndikuona kuti ndiri nazo

Njira 12 ____ Ndapeza zosowa zauzimu za pakhomu langa, mdera langa ndi mumpingo wanga

Njira 13 ____ Mphatso yanga ikugwirizana ndi zosowa ndipo ndi kukwaniritsa chosowachi.

Njira 14 ____ Ndaunikira utumiki wanga ndipo ndazindikira kuti ndi wamphamvu.

MAFUNSO A MPHATSO ZAUZIMU.

Pali mafunso amitundu iwiri okhudza mphatso zauzimu. Ena amakhudza mphatso yapadera ya utumwi, mneneri, mlaliki m'busa ndi mphunzitsi. Mafunso enawo amakhudza mphatso zauzimu zina zonse kupatula zimene zatchulidwa kale. Muyenera kuyankha mafunso okhudza mphatso zauzimu poyankha Eya kapena Ayi poyankha mafunsowa.

Chitsanzo:

Eya Ayi

(X) () 1. Kodi mukukhulupirira kuti Mulunguakukuitanani kuutsogoleri?

MAFUNSO OKHUDZA MPATSO ZAPADERA:

Mafunso awa akhazikika pa mphatso zapadera monga izi (Mtumwi, mneneri, mvangeri, m’busa ndi mphunzitsi. Mafunso awa apangidwa ndi cholinga choti akuthandizeni kuti muthe kuzindikira ngati muli ndi mphatso zimene zatchulidwezi. Ngakhale kuti maphunziro ndi othandiza, izi sizikuthauza kuti maphunzirowa akuysankha kunso linalilironse. Kotero, muyener kuunikira maitanidwe a Mulunguamene mukumva mkati mwanu. Ndi zofunika kuti mupitire kugwiritsa ntchito mphatso yanu moyenera komanso anthu ena ayenera kuchitira umboni z mphatso yanu.

Eya Ayi

- () () 1. Kodi mukukhulupirira kuti Mulungu akukuitanani ku utsogoleri?
- () () 2. Kodi mukukhumba mutakhala wa mishoni?
- () () 3. Kodi mukukhulupirira kuti Muli ndi kuthekera kolankhula kugulu la anthu?
- () () 4. Kodi muli ndi chikhumbokhumbo cholalikira uthenga Kwa anthu ena?
- () () 5. Kodi mumasangalatsidwa ndi kuwerenga Baibulo?
- () () 6. Kodi muli ndi khumbokhumbo lotumikira ngati ntchito yatsiku ndi tsiku?
- () () 7. Kodi mumakondweretsedwa ndi kuyenda malo osiyanasiysana?
- () () 8. Kodi mumaona kuti muli ndi kuthekera kolankhula ku khamu la anthu ambiri?
- () () 9. Kodi mumakondweretsedwa ndi kulalika uthenga wabwino kwa anthu osapulumsidwa kusiyana ndi kuphunzitsa akhristu?
- () () 10. Kodi mukhoza kukwanitsa kugwira ntchito ndi mpingo waung’ono kusiyaba ndi kupita malo kukafuna mwayi?
- () () 11. Kodi mumakulupirira kuti ukwati wanu kapena Banja n lachitsanzi chabwino chimene anthu ena akhoza kutsata?
- () () 12. Kodi mumamva kuti Muli ndi chidwi chachikulu chosura atsogoleri a mpingo?
- () () 13. Kodi mumatha kuona zinthu zimene ndi zolakwika ndipo mumalalakalaka mutakonzazithuzo?
- () () 14. Kodi kuchitira umboni kwa ophunzira kumakhala kosavuta kwa inu?
- () () 15. Kodi mumakondweretsedwa ndi maubale ndi anthu amene simumadziwana nao kwambiri.?
- () () 16. Kodi anthu ena amene amakudziwani akhoza kukufotokozani inu ngati munthu odekha komanso wachifundo?
- () () 17. Kodi munayambapo utumuiki otumikira Mulungu ndipo kuti anthu ena anaphunzitsidwa kuchita zimene Mumachita?
- () () 18. Kodi mumakamizidwa kuti Mulankhule mau a Mulungu kwa anthu amene ali munyengo zofunika mawu?
- () () 18. Kodi mumachitira umboni za Yesu chifukwa chakuti ndi udindo wanu kapena kuti chifukwa chakuti muli ndi chidwi?
- () () 20. Kodi mumakonda kugwira ntchito ndi anthu, mwina kuthandiza kuthana ndi mavuto awo, nkhawa zao, ndi mafunso awo?
- () () 21. Kodi mukhoza kudzifotokoza nokha ngati munthu amene ali ndi mwambo?
- () () 22. Kodi simumaona chovuta kukhala pakati pa anthu ena osiyana nao chikhalidwe?

- () () 23. Kodi munayamba mwamva okhulupirira ena akuichitira ndemanga kuti mukalankhula mau a Mulungu anthu ambiri amakhudzika?
- () () 24. Kodi wina anayamba wakuuzani kuti muli ndi mphatso ya mvangeri?
- () () 25. Kodi mukhoza kukondwera mutakhala kuti mwakhazikika pa utumiki ophunzitsa okhulupirira okhwima m'magawo osiyanasiyana?
- () () 26. kodi mukhoza kudzifotokoza nokha ngati munthu amane amadziwa kuchereza alendo kapena amene amakondwera kukhala pakati pa anthu?
- () () 27. Kodi ndinu munthu amene amatha kupirira nyengo zowawitsa?
- () () 28. Kodi ndinu munthu amene amatentheka mtima kuti mulalikira uthenga wabwino kwa anthu ngakhale musanauzidwe kuti mutero?
- () () 29. Kodi mumakhudzidwa komanso kukhala ndi chidwi chachikulu kuti mufikire ndi uthenga wabwino anthu amene sanapulumutsidwe?
- () () 30. Kodi mumamva mkati mwanu kuti muli ndi udindo oti muphunzitse okhulupirira ena kagwiritsidwe ka mphatso zauzimu moyenera?
- () () 31. Kodi ndinu munthu amene amatha kukhala bwinobwino ngakhale Pali mavuto azachuma kapena kuti pamene pali ndalana zochepa koma ndikukhala opanda nkhawa komanso osakhala ndi chilakolako choti mupange ndalama zambiri?
- () () 32. Kodi Mulibe udindo wina ulionse wapabanja kapena okhudza chithandizo chandalama umene ukhoza kukulepheleretsani kupita dziko lina kapena kukakhala pakati pa anthu achikhalidwe china?
- () () 33. Kodi mumakonda kulankhula kugulu la anthu kapena kulankhula ndi anthu paokhapaokha?
- () () 34. Kodi nthawi zambiri mumafunafuna mwayi oti mutumikire za Yesu Khristu?
- () () 35. Kodi simumaona vuto kutenga nthawi yanu yambiri kuchita kafukufuku kapena kuweringa Baibulo?
- () () 36. Kodi mwakhala Khristu kuposa dzaka zitatu?
- () () 37. Kodi mumakhulupirira kuti mukhoza kukopa anthu kubwera kwa Yesu ndikuwakonzeke kakhala abusa?
- () () 38. Kodi munayambapo mwalalikira ku gulu la anthu amane anasonkhana ndicholinga choti muwalalikire?
- () () 39. Kodi mumayamba tsikunditsiku ndi chiyembekezo komanso chikhumbokhumbo choti mulalikire Uthenga Wabwino kwa anthu osakhulupirira?
- INDE AYI
- () () 40. Kodi wina anayamba wakuuzanipo kuti mukhoza kukhala mphunzitsi kapena mlaliki wabwino?
- () () 41. Kodi munayamba mwakhalapo ndi udindo oyendetsa banja kapena malonda kotero kuti anthu ena okhoza kunena kuti munayendetsa zinthu bwino?
- () () 42. Kodi simaona chovuta chilichonse kukumana ndi anthu achilendo ndi kuyamba kudziwana nao?
- () () 43. Kodi mumakhudzidwa ndi makhalidwe amunthu kotere kuti mumakhala ndi chikumbokhumbo chotsutsana ndi makhalidwe osakhala bwino?
- () () 44. Kodi nthawi zambiri mumakhala ndi mwayi olankhula za Yesu ndi anthu osakhulupirira?

- () () 45. Kodi mumakhakhulupirira kuti Mulungu wakupatsani kuthekerera kotha kukonza mavuto a anthu munjira yoyenera?
- () () 46. Kodi muli ndi chikhulupiriro kuti okhulupirira ena akhoza kunena kuti muli ndi mpatso yautsogoleri.
- () () 47. Kodi kumakhala kosavuta Kwa inu kusiyira utsogoleri anthu ena amene aonetsera kuthekerera kotsogolera?
- () () 48. Kodi mukuona ngati anthu ena akhoza kukufotokozani ngati munthu amene amadziwa kulankhula pagulu la anthu?
- () () 49. Kodi mukhoza kunena kuti mumakhala ndi chilakolako chachikulu chautumiki kwa anthu osapulumsidwa kotero kuti izi zimaonekera muzimene mumakamba
- () () 50. Kodi mukhoza kusangalatsidwa ndi udindo osamala zosowa za anthu ena?

Kapezedwe ka Mphatso Yanu

Pamene mwamaliza kuyankha mafunso ali mumtundawa, malizitsani kuyankha mafunso ali pansywa kuti mudziwe mphatso yanu. Funso linalilironse limene munayankha kuti Eya, mukwathe mkhati mwakabokosi kamene kakuumilira nambala ya funso limene munayankha kuti eya. Zindikirani kuti simukuyenera kukhwatsha mafunso amene simunayankhe kuti eya. Mukuyenera kukhwatsha mafunso okhao amene munayankha kuti Eya.

Chitsanzo: Munthu uyu anayankha kuti Eya mafunso 1,6, ndi 13. Chifukwa chaichi, iye anakhwatsha mumabokosi amene muli manambala amafunso amene anayankha.

ZOMUYENEREZA MUNTHU.

Izi zimagwira ntchito kwa anthu	MNENERI
onse anayi amene ali ndi mphatso	(mlaliki)

(x) #1 () #3

(x) #6 () #8

() #11 (x) #13

Munthuyu anayankha mafunso 11, 3 ndi 8 kuti AYI. Chifukwa chaichi, iye sanakhwathe mafunso amenewa. Tsopano lembani mayankho anu kumafunsowa malinga ndi malangizo mwapatsidwa.

ZOMUYENEREZA MUNTHU

MNENERI

Izi zimagwira ntchito pa anthu onse

(Mlaliki)

Anayi amene ali ndi mpatso

- | | |
|------------------------------|------------------------------|
| <input type="checkbox"/> #1 | <input type="checkbox"/> #3 |
| <input type="checkbox"/> #6 | <input type="checkbox"/> #8 |
| <input type="checkbox"/> #11 | <input type="checkbox"/> #13 |
| <input type="checkbox"/> #16 | <input type="checkbox"/> #18 |
| <input type="checkbox"/> #21 | <input type="checkbox"/> #23 |
| <input type="checkbox"/> #26 | <input type="checkbox"/> #28 |
| <input type="checkbox"/> #31 | <input type="checkbox"/> #33 |
| <input type="checkbox"/> #36 | <input type="checkbox"/> #38 |
| <input type="checkbox"/> #41 | <input type="checkbox"/> #43 |
| <input type="checkbox"/> #46 | |
| <input type="checkbox"/> #48 | |

(

MTUMWI

MVANGELI

M'BUSA MLALIKI

(wamishoni)

- | | | |
|------------------------------|------------------------------|------------------------------|
| <input type="checkbox"/> #2 | <input type="checkbox"/> #4 | <input type="checkbox"/> #5 |
| <input type="checkbox"/> #7 | <input type="checkbox"/> #9 | <input type="checkbox"/> #10 |
| <input type="checkbox"/> #12 | <input type="checkbox"/> #14 | <input type="checkbox"/> #15 |
| <input type="checkbox"/> #17 | <input type="checkbox"/> #19 | <input type="checkbox"/> #20 |
| <input type="checkbox"/> #22 | <input type="checkbox"/> #24 | <input type="checkbox"/> #25 |
| <input type="checkbox"/> #27 | <input type="checkbox"/> #29 | <input type="checkbox"/> #30 |
| <input type="checkbox"/> #32 | <input type="checkbox"/> #34 | <input type="checkbox"/> #35 |
| <input type="checkbox"/> #37 | <input type="checkbox"/> #39 | <input type="checkbox"/> #40 |
| <input type="checkbox"/> #42 | <input type="checkbox"/> #44 | <input type="checkbox"/> #45 |
| <input type="checkbox"/> #47 | <input type="checkbox"/> #49 | <input type="checkbox"/> #50 |

MPATSO ZAPADERA

Pogwiritsa ntchito mayankho amene mwapereka pamwambawa, yankhani mafunso ali muniwa kuti muzindikire mpatso yanu yapadera. Werengani mabokosi amene munakhwacha pansa pa mophatso Ina iliyonse.

Chitsanzo: Umu ndi mnene munthu wina anayankhira mafunso ake:

ZOMUYENEREZA MUNTHU	MNENERI (MLALIKI)	
<input type="checkbox"/> #1	<input type="checkbox"/> #3	
<input checked="" type="checkbox"/> #6	<input type="checkbox"/> #8	
<input type="checkbox"/> #11	<input type="checkbox"/> #13	
<input type="checkbox"/> #16	<input checked="" type="checkbox"/> #18	
<input checked="" type="checkbox"/> #21	<input type="checkbox"/> #23	
<input checked="" type="checkbox"/> #26	<input type="checkbox"/> #28	
<input checked="" type="checkbox"/> #31	<input checked="" type="checkbox"/> #33	
<input type="checkbox"/> #36	<input type="checkbox"/> #38	
<input type="checkbox"/> #41	<input checked="" type="checkbox"/> #43	
<input type="checkbox"/> #46	<input checked="" type="checkbox"/> #48	
Mtumwi	Mlaliki	m'busa ndi mphunzitsi
<input type="checkbox"/> #2	<input checked="" type="checkbox"/> #4	<input checked="" type="checkbox"/> #5
<input checked="" type="checkbox"/> #7	<input checked="" type="checkbox"/> #9	<input type="checkbox"/> #10
<input checked="" type="checkbox"/> #12	<input checked="" type="checkbox"/> #14	<input type="checkbox"/> #15
<input type="checkbox"/> #17	<input checked="" type="checkbox"/> #19	<input checked="" type="checkbox"/> #20
<input checked="" type="checkbox"/> #22	<input checked="" type="checkbox"/> #24	<input type="checkbox"/> #25
<input type="checkbox"/> #27	<input type="checkbox"/> #29	<input type="checkbox"/> #30
<input checked="" type="checkbox"/> #32	<input checked="" type="checkbox"/> #34	<input type="checkbox"/> #35
<input checked="" type="checkbox"/> #37	<input checked="" type="checkbox"/> #39	<input type="checkbox"/> #40
<input type="checkbox"/> #42	<input checked="" type="checkbox"/> #44	<input type="checkbox"/> #45
<input type="checkbox"/> #47	<input checked="" type="checkbox"/> #49	<input type="checkbox"/> #50

Umu ndi mmene mpatso zao zingaonekere pagarafu

Wina aliyense



Mtumwi



Mneneri



|

Mvangeri



M'busa/mphunzits



|

1 2 3 4 5 6 7 8 9 10

Mzere wautali uja ukuimilira malikisi ambiri

Mzere waufupi ukuimilira malikisi ochepa

Tsopano gwiritsani ntchito mayankho anu aja kuti mupeze malikisi anu kapena chimene muli.

MPHATSO ZAPADERA

Wina aliyense

Mtumwi

Mneneri

|

Mvangeri

M'busa/mphunzitsi

|

1 2 3 4 5 6 7 8 9 10

Mzere wautali uja ukuimilira malikisi ambiri

Mzere waufupi ukuimilira malikisi ochepa

MPHATSO ZAUZIMU

MAFUNSO OKHUDZA MPATSO ZAUZIMU

EYA INDE

- () () 1. Kodi mukhoza kudzifotokoza ngati munthu amene amadziwa kulakhula bwino kugulula kwa anthu?
- () () 2. Kodi mumakondweretsedwa ndi kusanthula Baibulo mozama kapena kuchita kafukufuku wa Bibulo?
- () () 3. Kodi mumakondweretsedwa kugawana nkhwana ndi anthu ena?
- () () 4. Kodi mumakhala ndi chidwi chogwiritsa ntchito mfundo zimene Baibulo limafotokoza kapena mumangondweretsedwa ndi kumvetsetsa Baibulo?
- () () 5. Kodi mumatha kuzindikira kuthekera kumene muli nako kokwanitsa kuphunzira mozama Mau a Mulungu?
- () () 6. Kodi mumakonda kulimbikitsa anthu ena kuchita mautumiki osiyanasiyana?
- () () 7. Kodi anthu ena akhoza kukufotokozani kuti mumatha ziganizo mosavuta?
- () () 8. Kodi mumakondweretsedwa ndi kungochita zinthu osati zifukwa zimene zinthu zoyenera kuchitika?
- () () 9. Kodi mukaona munthu amene akufunika chithandizo mumachitapo kathu kuti muthandize?
- () () 10. Kodi mukhoza kukonda kuthandiza ndi ndalama kusiyana ndi kugwira ntchito ndi manja anu?
- () () 11. Kodi mumakondweretsedwa ndi kuyendera anthu odwala?
- () () 12. Kodi nyumba yanu ndi khomo limene anthu ambiri akhoza kukhala omasuka kukuyenderani?
- () () 13. Kodi muli ndi kuthekera kokhulupirira zinthu zimene anthu ena kukhoza kukhala kovuta kukhulupirira?
- () () 14. Kodi anthu ena anayamba akuuzani kuti mumadziwa ngati chinthu chili cholondora kapena cholakwikwa?
- () () 15. Kodi pamene zinthu zikulakwikwa mumamva kulemera mkati mwanu kuti muchitepo kanthu?
- () () 16. Kodi mumakonda kuyankha mafunso kapena kufotokozerana zinthu?
- () () 17. Kodi munayamba mwazindikira kuti anthu nthawi zambiri amabwera kwa inu kufuna uphungu pamavuto awo?

- () () 18. Kodi mumapezeka kuti mukudziwa chimene mukuyenera kuchita munyengo imene ena sakudzidwa chimene ayenera kuchita?
- () () 19. Kodi zinayamba zakuchitikirani kuti anthu nthawi zonse amabwera kwa inu ndi mafunso ovuta okhudza Baibulo kuti amve mamvetsetsedwe anu?
- () () Kodi mumakhazikitsa zinthu zofuna kukwanitsa zokhudza inu mwini kapena utumiki inu ngati munthu okhulupirira.?

INDE AYI

- () () 21. Kodi mumatha kuona kuti muli ndi udindo waukulu opanga ziganizo mmalo mwa anthu ena?
- () () 22. Kodi mumapeza chimwemwe pochita zinthu zimene zikuyenera kuchitika posatengera kuti zinthuzo ndi zazing'ono bwanji?
- () () 23. Kodi mumatha kuona utumiki wapadera othandiza anthu ena kuti akhale atumiki amphamvu?
- () () 24. Kodi mukamva munthu akuvutika, mumalingalira zothandiza nthawi yomweyo ndi ndalama?
- () () 25. Kodi mukamva kuti munthu akuvutika muchipatala, kodi mumasunthika kuti mumulimbikitse munthuyo?
- () () 26. Kodi mumava kupelewera mukhala kuti simukulandira alendo panyumba panu?
- () () 27. Pamene anthu akunena kuti chinthu chinachake sichingachitike, kodi inu mumakhulupirira Mulungu kuti akhoza kuchitabe?
- () () 28. Kodi mumakhala ndi kumvetsetsa anthu ngakhale zimukuwadziwa bwinobwino?
- () () 29. Kodi muli ndi chizolowezi cholakhula pamene nkhani ikukambidwa pagulu kusiyana ndi kukhala chete ndikumvetsera?
- () () 30. Kodi mukamva funso mukhala ndi mtima oti mupeze ndi kupereka yankho?
- () () 31. Kodi mumatha kukamba ndi munthu zamavuto ake kapena mumauza anthu ena kuti awathandize?
- () () 32. Kodi nthawi zambiri mumafunafuna uphungu pa zoti muchite munyengo zovuta?
- () () 33. Pamene muwerenga mau a Mulungu, kodi zimakhala zosavuta kuzindikira kamvetsetsedwa kwatsopano kwa mau a Mulungu?
- () () 34. Kodi pamene munthu wina sakuchita bwino ntchito yake, mumakhala okhudzika kuti munthandize munthuyo kuti achite bwino?
- () () 35. Kodi mumakhudzika pamene mukupereka uphungu ndi mmene uphunguwo ungakhudzire munthu?

- () () 36. Kodi mumakhala okhutitsidwa ndikuchita zinthu kusiyana ndi zimene anthu akuganiza kuti muchite?
- () () 37. Kodi mumadziona nokha ngati munthu ongothandizira utsogoleri wa ena osati kuti unuyo ndi mtsogoleri?
- () () 38. Kodi mumatha kukwanitsa kufunafuna koti mupereke ndalama zanu kusiyana ndi kuchita kudikira kupemphedwa kuti muthandize?
- () () 39. Kodi zimakhala zosavuta kwa inu kuonetsa chimwemwe kwa anthu amene akuvutika kuthupi?
- () () 40. Kodi mumakonda kulandira alendo mnyumba mwanu posatengera kuti mumawadziwa kwambiri?

Eya AYI

- () () 41. Kodi mumaona ngati munthu akutsutsana nanu pamene akunena kuti zinthu sizingatheke kapena kukwaniritsidwa?
- () () 42. Kodi nthawi zambiri mumatha kuzindikira kuti zimene zikukambidwa zikuchokera kwa Satana osati Mulungu ndipo izi mapeto ake zimakhala zolondora?
- () () 43. Kodi muyamba mwazindikira kuti anthu amakhudzidwa ndi zinthu zolakwikwa pamene mugawana nao zimene Baibulo limaphunzitsa?
- () () 44. Kodi anthu anayamba akuuzani kuti muli ndi kuthekera kofotokoza zinthu zovuta kapena mavuto ovuta kwa anthu?
- () () 45. Kodi mumakondewera ndi kuthandiza anthu amene akukumana ndi mavuto komanso mayesero?
- () () 46. Kodi nthawi zambiri anthu amakhala akubwera kwa inu kudzafunsa mzeru?
- () () 47. Kodi munazindikira kuti muli ndi kuthekera komvetsa mau a Mulungu mwansanga osachita kulira kuwerenga mozama kapena kuchita kafukufuku?
- () () 48. Kodi mukhoza kukonda kumuonetsa munthu kachitidwe kachinthu kusiyana ndi kuchita nokha chinthucho?
- () () 49. Kodi mumakondwera ndi kupereka chitsogozo kwa anthu ena kuti apange ziganizo?
- () () 50. Kodi ndi zoona kuti mukauzidwa kuti mupange chinthu simmaona vuto kapana sim'maona kuti ndi udindo wanu?
- () () 51. Kodi mumakondweretsedwa kuthandiza anthu ena kukwanitsa kuchita ntchito yawo kuti apepukidwe ndi kuchita ntchito zina?

- () () 52. Kodi mumakwanitsa kuchita zinthu zofuna ndalama nthawi zonse osachita kulira dongosolo lapadera?
- () () 53. Kodi Kumakhala kophweka kwa inu kulakhura ndi anthu zokhudza mavuto awo akuthupi?
- () () 54. Kodi mumaona khomo lanu ngati malo autumiki?
- () () 55. Kodi mumadziwa kuti simukuyenera kupeza umboni ogwirika weniweni kuti mupange chiganizo?
- () () 56. Kodi nthawi zambiri mumakhala mukuunikira zonenena za anthu ngati zili z olondora kapena ayi.
- () () 57. Pamene mulalikira mau a Mulungu kodi mumalingalira mmene mauwo angakhudzire anthu?
- () () 58. Kodi anthu anayamba akuuzani muti amakondwera ndi mmene mumafotokozerana mfundo za Baibulo?
- () () 59. Kodi mumaona kosavuta kuthandiza anthu amene ndi okhumuditsidwa kuti athe kuzindikira chimwemwe chimene akhoza kupeza?
- () () 60. Kodi munayamba mwauzidwapo ndi okhulupirira ena kuti chiganizo chimene munapanga chinali choyenerako komanso chabwino.

INDE AYI

- () () 61. Kodi mumatha kumvetsa zinthu zokhudza mau a Mulungu zimene okhulupirira ena ngati inu samatha kumvetsa?
- () () 62. Kodi mumakhudzika ndi kuphunzitsa okhukupirira ena kuti akhale atsogoleri?
- () () 63. Kodi nthawi zonse mumakhala mukulingalira za ziganizo zimene ziyenera kupangidwa kuti zinthu ziyenge pa gulu la anthu kapena pa bungwe limene?
- () () 64. Kodi mukhoza kukonda kugwira ntchito nokha kapena ndi gulu la anthu kuti mukwaniritse ntchitoyo?
- () () 65. Kodi mumakhulupirira kuti mukhoza kuthandiza kutakhala kotero?
- () () 66. Kodi mumapeza chimwemwe pamene mupereka posatengera zimene olandirayo angakupangireni?
- () () 67. Kodi nthawi zambiri mumakhala mukuganiza njira zimene mungathandizire anthu ovutika kuthupi?
- () () 68. Kodi mungakonde mutakhala ndi utumiki olandira alendo mnyumba mwanu posatengera kuti ndi ndani?
- () () 69. Kodi mukhoza kukhulupirira chinthu chinachake pamene anthu onse sakukhulupirira?

- () () 70. Kodi mumatha kuzindikira udindo wanu Kwa Mulungu pamene zinthu sizili bwino ngakhale kuti okhulupirira ena asamvetsetse?
- () () 71. Kodi munauzidwapo ndi okhulupirira ena kuti muli ndi kuthekera kolalika mau a Mulungu mwamphamvu?
- () () 72. Kodi anthu amabwera kwa inu kudzafuna uphungu kapena mayankho amavuto awo?
- () () 73. Kodi mumaonetsera chikondi komanso kukhudzika ndi anthu amene ali ndi nkhawa?
- () () 74. Pamene mupereka uphungu kwa munthu, kodi mumatsindika mmene munthuyo ayenera kuchitira kapena zifukwa zimene munthuyo ayenera kutsatira uphunguwo?
- () () 75. Kodi okhulupirira ena anayamba akuuzani kuti muli ndi kuthekera komvetsetsa mau a Mulungu?
- () () 76. Kodi mumakhudzika ndi kuthandiza anthu kuti akwanitse zolinga zawo zamoyo?
- () () 77. Kodi anthu amadalira inuyo kuti apange ziganizo zikuluzikulu zokhudza gulu la anthu kapena bungwe?
- () () 78. Pakakhala kuti pali ntchito yoti ichitike, Kodi mumakhudzika kuti ntchitoyo muyichite nokha?
- () () 79. Kodi mumakhutitsidwa ndi mmene munthu wathandiziridwa kapena mumakhutitsidwa ndikuthandiza munthuyo?
- () () 80. Pamene mwapereka ndalama, kodi mumapewa kuti anthu ena asadziwe zimene mwachitazo?

Eya Inde

- () () 81. Kodi mukhoza kukondweretsedwa ndi utumiki okhazikika othandiza nthu amene akuvutika kuthupi?
- () () 82. Kodi mumaona kulandira alendo pakhomo panu ngati utumiki osangalatsa osati ngati udindo chabe?
- () () 83. Kodi munayamba mwauzidwapo ndi okhulupirira ena kuti mumkhala ndi chikhulupiriro mwa Mulungu ngakhale mu nyengo zowawa
- () () 84. Kodi anthu anayamba akufusanipo za maganizo pa munthu winawake kapena zinthu zinazake ndipo maganizo anu anali olondora?
- () () 85. Kodi mumakhulupirira kuti muli ndi mpatso yodziwa kulankhula ndi anthu?
- () () 86. Kodi mumatha kufotokozerana tanthauzo la mau kapena mumadziwa kungotchula vesi kwa munthu?

- () () 87. Kodi mumakondweretsedwa kumva mavuto a anthu ena kuyisana ndi kuuza anthu ena zamavuto anu?
- () () 88. Kodi okhulupirira ena amatha kutsata uphungu wanu munyengo zovuta?
- () () 89. Kodi munazindikira kuti mumatha kudziwa chimene ndime ikunena ena asandizindikire pamene mukusanthula mau a Mulungu ndi ophunzira ena?
- () () 90. Kodi mumakwanitsa kutenga utsogoleri pagulu limene lilibe utsogoleri?
- () () 91. Kodi mumaona kuti muli ndi udindo pa zotsatira zimene zingabwere mtsogolo chifukwa cha ziganizo zanu?
- () () 92. Kodi mukhoza kukonda kugwira ntchito ina yake kusiyana ndi kugwiritsa ntchito nthawi yanu kulankhula ndi anthu zamavuto awo?
- () () 93. Kodi zimakhala zokuvutani kuti munene ayi pamene munthu wakupemphani kuti mumuthandize?
- () () 94. Pamene mwapereka ndalama kwa munthu, kodi simumayembekezera kuthokozedwa kulikonse?
- () () 95. Kodi mumatha kuona kuti mukhoza kukwanitsa kulandira alendo kunyumba kwanu koma osaona chovuta chinachilichonse?
- () () 97. Kodi mumamva mkati mwanu kuti mukuyenera kulimbikitsa anthu kuti akhulupirire Mulungu pamene akudutsa munyengo zowawa?
- () () 98. Kodi mumaona kuti muli ndi udindo wapadera kuti muteteze choonadi cha mau a Mulungu podzudzura poyera zinthu zolakwika komanso zauchimo?
- () () 99. Kodi mukhoza kukonda kulakhula mau a Mulungu kwa anthu kusiyana ndi kufotokozera mwatsatanitsatani?
- () () 100. Kodi zimene mumaganiza zimakhala zandondomeko?
- () () 101. Kodi mumakhala ndi mtima oti muthandize pamene mwaona kuti munthu okhulupirira wachimwa?
- () () 102. Kodi uphungu ndi malandizo umene munapereka munthawi yamavuto unayamba wakhalapo olondora?

Eya Inde

- () () 103. Kodi munkhaka ndi chidwi chofuna kugawana ndi okhulupirira ena ndime zovutsa za m'baibulo?
- () () 104. Kodi mumakhala ndi chimwemwe kutenga udindo wautsogoleri, kapena kuti zimakhala zovuta komanso zokhumudwitsa kutero?
- () () 105. Kodi munayambapo mwakhala ndi udindo opanga chiganizo chokhudza gulu la anthu kapena bungwe?

- () () 106. Kodi mumakondwera kuchita zinthu osachita kudikira kuuzidwa kuti muchite zinthu?
- () () 107. Kodi mumafunafuna mwayi oti muthandize anthu ena?
- () () 108. Kodi mumaona ngati kupereka ndalama ndi utumiki wauzimu umene Mulungu anakupatsani?
- () () 109. Kodi kuyendera anthu amene akuvutika kuthupi ndi chinthu chimene mumakondera nacho kapena chimakusowetsani mtendere.
- () () 110. Kodi okhulupirira ena anayamba akuuzani zakuthekera kwanu kumene mumaonetsa polandira alendo kunyumba kwanu komanso mmene Mulungu amakugwiritsilirani ntchito kuchita izi?
- () () 111. Kodi munaonapo Mulungu akupanga zinthu zimene anthu ena amati sizingatheke koma inuyo mumakhulupirira Mulungu kuti akhoza kuchita?
- () () 112. Kodi mumaona kuti mukuthandiza pamene mwazindikira kuti chinachake ndi cholakwika ndipo iwonso avomereza?
- () () 113. Pamene mwapatsidwa mwayi oti mulankhule mau a Mulungu, kodi mumaona chophweka kugawana mavesi ndi anthu aja kapena zinthu zimene mwakumana nazo?
- () () 114. Kodi okhulupirira ena anayamba akuuzanipo kuti muyenera kuyamba utumiki ophunzitsa okhazikika ndipo inunso mumaona chimodzimodzi?
- () () 115. Kodi mumakondwera kutumikira munthu payekhapayekha kusiyana ndi kutumikira gulu la anthu?
- () () 116. Kodi mumadziwa kuti muli ndikuthekera kothana ndi mavuto akuluakulu?
- () () 117. Kodi mumaona kuti muli ndi udindo ofotokozera okhulupirira amene sakumvetsetsa Baibulo kuti amvestse ziphunzitso zina zovuta kumvetsetsa?
- () () 118. Kodi mumatha kuthandiza zosowa za anthu posafuna kutenga nthawi yambiri yopanga dongosolo?
- () () 119. Kodi mumakondwera kukhala munthu otsogolera anthu kapena bungwe la anthu limene likuchita bwino?
- () () 120. Kodi mumaona kufunika kouzidwa chochita pamene mwapatsidwa chochita?
- () () 121. Kodi munayamba mwauzidwapo kuti mwawapepuza anthu ena kuchita ntchito yawo kuti anthe kupanga zinthu zina?

Eya Ayi

- () () 122. Kodi mumakondwera pamene anthu ena akupemphani kuti muwathandize kumbali ya zachuma pazochitachita zao ndipo kodi izi munazona ngati ulemu wapadera?
- () () 123. Kodi ndinu okonzeka kugwiritsa ntchito zinthu zanu monga ndalama ndi cholinga chothandiza anthu amene akuvutika kuthupi?
- () () 124. Kodi mumakondwera kulandira anthu ambiri panyumba panu kapena ichi mumachiona ngati chinthu chovuta kwambiri?
- () () 125. Kodi munazindikira utumiki wamphamvu wamapemphero umene mayankho pa umunthu amaoneka ngati osatheka koma ndi pemphero zimatheka?
- () () 126. Kodi munayambapo mwaunikirapo munthu kapena chinthu chinachake ndipo zotsatira zake ndikukhaladi zoona?

KUZINDIKIRA MPHATSO ZANU:

Pamene mwamaliza kuyankha mafunso ali mwambawa, yankhaninso mafunso mafunso ali munsiwa, khwatchani mkati mwabokosi la funso linalilironse limene mwayankha kuti eya. Koma simukuyenera kukhwatcha mkati mwafunso limene simunayankha

UNENERI	MAU A LUNTHA	KUYENDE TSA ZINTHU	KUPEREKA	CHIKHULUPIRIRO
() #1	() #4	() #7	() #10	() #13
() #15	() #18	() #21	() #24	() #27
() #29	() #32	() #35	() #38	() #41
() #43	() #46	() #49	() #52	() #55
() #57	() #60	() #63	() #66	() #69
() #71	() #74	() #77	() #80	() #83
() #85	() #88	() #91	() #94	() #97
() #99	() #102	() #105	() #108	() #111
() #113	() #116	() #119	() #122	() #125
KUPHUNZITSA	MAU ACHIDZI WITSO	KUTUMIKILA	KUONETSA CHIFUNDO	CHIDZI WITSO
() #2	() #5	() #8	() #11	() #14

() #16	() #19	() #22	() #25	() #28
() #30	() #33	() #36	() #39	() #42
() #44	() #47	() #50	() #53	() #56
() #58	() #61	() #64	() #67	() #70
() #72	() #75	() #78	() #81	() #84
() #86	() #89	() #92	() #95	() #98
() #100	() #103	() #106	() #109	() #112
() #114	() #117	() #120 ()	() #123	() #126

EXHORTATION	UTSOGOLERI	KUTHANDIZA	KUCHELEZA ALENDO
() #3	() #6	() #9	() #12
() #17	() #20	() #23	() #26
() #31	() #34	() #37	() #40
() #45	() #48	() #51	() #54
() #59	() #62	() #65	() #68
() #73	() #76	() #79	() #82
() #87	() #90	() #93	() #96
() #101	() #104	() #107	() #110
() #115	() #118	() #121	() #124

KUONKHETSERA ZANU ZAUZIMU MPHATSO ZAUZIMU:

Pogwiritsa ntchito mayanko amene alembedwa pa tsamba la pamtundali, okhotserani mphatso zanu zauzimu pa tsamba lili munsiri. Pa mphatso ina iliyose, werengani mabokosi amene mwayankha kuti eya. Jambulani mizere ndipo mphatso ina iliyonse iyenera kukhala ndi mzere wake

Uneneri

Kuphunzitsa

Kulimbikitsa

Mau a luntha

Mau achidziwitso

Utsogoleri

Kuyendetsa zinthu

Kutimikira

Kuthandizira

Kupereka

Kuonetsa chifundo

Kuchereza alendo

Chikhulupiriro

Chidzitso

1 2 3 4 5 6 7 8 9 10

Nzere umene ndi wautali pa galafu yanu ukuonetse mphatso imene mwachita bwino kapena kuti imene ili ndi malikisi ambiri.

Mzere waufupi pa galafu yanu ukuimira mphatso zimene inuyo mulibe. Pali mphatso zambiri zimene sizinayikidwe pa mafunsowa koma ngati muli nazo mphatsozi, zizindikiro zake ndi zodziwika kale.

CHAPUTALA 11

CHIPATSO CHA MZIMU WOYERA

Pamapeto pa chaputala ichi muyenera kukwaniritsa zinthi izi:

- Kuzindikira Chipatso chakunja cha Mzimu Woyera.
- Kuzindikira chipatso chamkati cha Mzimu Woyera.
- Kufotokoza kufunika kwa chipatso cha Mzimu Woyera.
- Kupeza mavesi owonetsera kuti tiyenera kubala chipatso.
- Kufotokoza zipatso zamkati zosiyanasiyana.
- Kusiyanitsa pakati mtender wa Mulungundi mtendere ndi Mulungu.

VESI YOTSOGOLERA:

Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, icikhulupirtro, cifatso, ciletso; pokana zimenezi palibe lamulo. (Agalatiya 5:22-23)

CHIYAMBI

Chaputala ichi chifotokoza za chipatso cha Mzimu Woyera. Chaputala chachiwiri tiphunzira zinthu zosiyana ndi chipatso chauzimu ndipo izi zimatchedwa ntchito zakuthupi. Chaputala chomaliza muphunzira mmene mungakuzire chipatso cha Mzimu Woyera.

KODI CHIPATSO NDI CHANI?

Chipatso cha Mzimu Woyera ndi chikhalidwe chimene chimaoneker m'moyo wa munthu okhukupirira. Kapena kuti ndi chikhakidwe chauzimu chimene chiyenera kuonekera m'moyo wa munthu okhukupirira.

Chipatso cha Mzimu Woyera ndi mphamvu komanso ndi chimene chimatipatsa makhalidwe. Chithuzi chili pansichi chikuonetsera kusiyana pakati pa mpatso zauzimu ndi chipatso chauzimu.

Mpatso	Chipatso
- Ndi za utumiki	kuti okhulupira akule
- Okhukupirira samakhala ndi mpatso zonse	Okhulupirira ayenera kukhala ndi zonse
- Kupereka mphamvu	kuti tikhale ndi khalidwe

Chipatso chazimu ndi umboni wakukhwima mu uzimu. Ndipo chimodzimidzi chipatso chamtengo wakuthupi umene chipatso chimaonetsera moyo. Chipatso chazimu ndi khalidwe lachikhristu limene timaonetsa ngati anthu kapena kwa anthu ena ndipo izi ndi zotsatira za Mzimu Woyera amene amagwira ntchito mkati mwathu. Chipatsop cha mtengo chimatenga nthawi kuti chikule ndipo izi ndi chimodzimidzi ndi chipatso chazimu chimene chimatenganso nthawi kuti chikule.

MITUNDU IWIRI YA CHIPATSO

Baibulo limafotokoza za mitundu iwiri ya chipatso chazimu:

1. Chipatso cha kulalika uthenga Wabwino.
2. Chipatso cha makhalidwe auzimu a umulungu.

Mzimu Woyera amathandiza okhulupirira kuti abale chipatso chowoneka ndi maso powapanga iwo kukhala mboni zauthenga Wabwino zamphamvu. Komanso Mzimu Woyera amathandiza kukuza chipatso chazimu chamkati chimene ndi chikhalidwe chofanana ndi Yesu Khristu.

CHIPATSO CHOWONEKERA KULARIKA

KUBALA KWA KUTHUPI:

Mulungu atalenga Adamu ndi Hava, Iye anawalamura iwo kuti abalane ndikulidzadza dziko lapansi.

Mulungu ndipo anadalitsa iwo, ndipo adati kwa iwo, Mubalane, mucuruke, mudzaze dziko lapansi, muligonjetse: mulumulire pa nsomba za m'nyanja, ndi pa mbalame za m'mlengalenga, ndi pa zamoyo zonse zakukwawa pa dziko lapansi. (Genesis 1:28)

Kudziko lakuthupi, Mulungu anakhazikitsa ndondomeko yakubala kopitirira:

Pakukhalabe masiku a dziko lapansi, nthawi yakubzala ndi yakukunkha, cisanu ndi mafundi, malimwe ndi msakasa, usana ndi usiku sizidzalekai.

KUBALA KU UZIMU:

Kuchokera pachiyambi, Mulungu analamura anthu ake kuti abale kuthupi ndi kuuzimu komwe. Adamu ndi Hava amayenera kubala kuthupi ndi kuuzimu komwe. Chikonzero cha Mulungu chapachiyambi chinali choti iwo amayenera kudzadza dziko lapanso ndi anthu olengedwa muchifaniziro cha Mulungu komanso kukhala pachiyanjano ndi Mulungu.

Pamene Mulungu anadzutsa fuko la Israeli ngati gulu la anthu limene Mulungu akhoza kuonetsera mphamvu yake komanso chikonzero chake cha dziko lapansi. Iye anawaitana iwo kuti akabale muuzimu:

Mudatenga mpesa kucokera ku Aigupto: Munapitikitsa amitundu ndi kuuoka uwu. Mudasoseratu pookapo, Idagwiritsa mizu yace, ndipo unadzaza dziko. Mthunzi wace unaphimba mapiri, Ndi nthambi zace zikunga mikungudza ya Mulungu. (Masalmo 80:8-10)

“Mpesa” umene Mulungu anatuluka nao mu Aigupto ndi fuko la Israeli. Iye amafuna kuti Israle abale chipatso chazimu pakuonetsera Mulungu weniweni pakati pa anthu a mitundu yosakhulupirira imene inawazungulira. Koma m'malo mwa izi, Israeli amakhala ngati amitundu. Iwo Anayamba kupembedza milungu yachilendo komanso amafuna kukhala ndi mfumu yowoneka ndi maso kuti ilamulire pakati pawo osati Mulungu ngati Mfumu yawo. Koma Mulungu anati kwa Israeli:

Israyeli ndi mpesa wotambalala, wodzibalira wokha zipatso; monga umo zinacurukira zipatso zace, momwemo anacurukitsa maguwa a nsem be ace; monga mwa kukoma kwace kwa dziko lace anapanga zoimiritisa zokoma. (Hoseya 10:1)

Chifukwa chosabala kuuzimu, Yesu anati:

Cifukwa cace ndinena kwa inu, 2 Ufumu wa Mulunguudzacotsedwa kwa inu, nudzapatsidwa kwa anthu akupatsa zipatso zace. (Mateyu 21:43)

Chifukwa chakuti Israeli anakanika kubala chipatso, Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu unaperekedwa kwa anthu amitundu. Kudzera mwa anthu amitundu, Mulungu anadzutsa mpingo ndi cholinga chofuna kukwaniritsa kubalana kuuzimu pa dziko lonse lapansi.

KUSANKIDWA KUTI MUBALE CHIPATSO:

Ngati anthu okhulupirira, Yesu watisankha kuti tibale chipatso pakufalitsa Uthenga Wabwino pa dziko lonse lapansi.

Inu simunandisankha Ine, koma Ine ndinakusankhani inu, ndipo ndinakuikani, kuti mukamuke inu ndi kubala cipatso, ndi kuti cipatso canu cikhale; kuti cimene ciri conse mukapempha Atate m'dzina langa akakupatseni inu. Lamulo lake lomaliza kwa ophunzira linali lokhudza kubala muuzimu: (Yohane 15:16)

Marko 16:15 Ndipo ananena nao, mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse. (Mark 16:15)

Iye anawatsikimizira ophunzira ake za masomphenya a kholora lauzimu:

Yohane 4:35-36 Kodi simunena inu, kuti, Yatsala miyezi inai, ndipo kudza kumweta? Onani ndinena kwa inu, Kwezani maso anu, nimuyang'ane m'minda, kuti mwayera kale kufikira kumweta. Wakumweta alandira kulipira, nasonkhanitsira cobala ku moyo wosatha; kuti wofesayo akakondwere pamodzi ndi womwetayo. (Yohane 4:35-36)

Solomoni anati:

**Cipatso ca wolungama ndi mtengo wa moyo; Ndipo wokola mtima ali wanzeru.
(Miyambi 11:30)**

Mphatso ya Mzimu Woyera imathandiza okhulupirira kuti abale zipatso kudzera mukulalika Uthenga Wabwino:

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. (Macitidwe 1:8)

Njira zakubala muuzimu zaperekedwa pa II Timoteo 2:2:

Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso. 2 Timoteo 2:2)

Mmene Mulungu anakhazikitsira nyengo ya kholora mu dziko lakuthupi, chimodzimidzinsu anakhazikitsa nyengo yakubala mudziko lauzimu. Okhulupirira wina aliyense akuyenera kuphunzitsa Uthenga Wabwimo kwa anthu ena amene naonso ayenera kuphunzitsa anthu ena. Nyengo yakufesa yakudziko ilibe malire ndipo izi ndi chimodzimidzi ndi nyengo yakubala kuthupi.

Chifukwa chakufunika kwa chipatso chooneka ndi maso chakufalitsa uthenga Wabwino, International Harvestime Institute ili ndiphunziro lapadera lokhudza *ndondomeko za Khololora: Njira zakuchulukitsa:*

CHIPATSO CHAMKATI: MOYO NGATI WA KHRISTU

Kuonjezera chipatso choonekera ndi maso cha kulalika uthenga wabwino, Baibulo limafotokoza zamakhalidwe amene amayenera kuonekera mwa okhulupirira chifukwa cha Mzimu Woyera. Chipatso chimenechi chimatchedwa chipatso chamkati chamoyo ngati wa khristu Yesu. Chipatso chimene chinatchulidwa pa Agalatiya 5:22-23:

Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, icikhulupirtro, cifatso, ciletso; pokana zimenezi palibe lamulo. (Agalatiya 5:22-23)

Izi ndi zipatso zamkati zimene Mzimu Woyera amafuna kukuza pamoyo wa okhulupirira. Awa ndi makhalidwe amene amaonekera mwa Khristu Yesu. Ichi ndi chifukwa chake makhalidwe amenewa amatchedwa makhalidwe ngati aYesu.

Mau oti chipatso amaonetsa chinthu chimodzi, samaonetsa zinthu zambiri. Koma muyenera kukumbukira kuti mphatso ndi zambiri ndipo zimagawidwa pakati pa okhulupirira malinga ndi chifuniro cha Mzimu Woyera. Chitanzo chabwino ndi cha nthochi. Mphava la nthochi limapangidwa ndi nthochi zambiri koma nthochi ina iliyonse imakhala kuti ili pa phava. Koma nthochi kaya imodzi kaya zambira imatchedwa nthochi basi.

Mu dziko lauzimu, chipatso chauzimu chili ngati mphva la nthochi. Paphava pamakhala nthochi zambiri zimene zimakhala pamodzi, chimodzimidziso mpatso zauzimu zosiyanasiyana zimakhala pamodzi ngati paphava. Ichi ndi chipatso chimodzi chakukula muuzimu chimene chimaonekera mumakhalidwe ngati a Yesu Khristu.

Chipatso chimodzi_____ Kukula Muuzimu

Makhalidwe abwino_____

Chifatso

mtendere ndi chikondi

Chifundo

Chipiriro

Kukhulupirira.

Cholinga cha Mulungu ndi chakuti okhulupirira akhale ndi chipatso cha Mzimu Woyera . Kusiyanana ndi mpatso zimene ndi zambiri komanso zosiyana pakati pa okhulupirira, chipatso chiyenera kukhala ndi okhulupirira wina aliyense.

Chipatso cha Mzimu Woyera chimaonekera muchina chirichonse chabwino, choonadi chimene chimachitidwa ndi okhulupirira.

pakuti cipatso ca kuunika ticipeza m'ubwino wonse, ndi cilungamo, ndi coonadi, (Aefeso 5:9)

CHIKONDI

Chikondi ndi kukhudzika kwakulu komanso chisamaliro. Ndikudzipereka kopanda malire kwa anthu ena posatengera nyengo zao kapena zimene akudutsamo. Monga mmene tinaonera kale, chikondi ndiye nsanamira ya mpatso zonse zauzimu. Mpatso zonse zauzimu zimakula chifukwa cha chikondi. Izi zimaonekera mukafananitsa ndime ya chipatso cha Mzimu Woyera yopezeka ku Agalatiya ndi ndime ya 1 Akorinto 13: 1-7 Agalatiya 5: 22-23

Chikondi cikhala choleza, ciri chokoma mtima; chikondi sichidukidwa; chikondi sici ziwa kudzitamanda, sici dzikuza, sici cita zosayenera, sici sata za mwini yekha, sici pisa mtima, sici lingirira zoipa; sici kondwera ndi cinyengo, koma cikondwera ndi coonadi; cikwirira zinthu zonse, cikhulupirira zinthu zonse, ciyembekeza zinthu zonse, cipirira zinthu zonse.

Chikhulupiriro, chimene ndi mpatso komanso chipatso cha Mzimu Woyera chimagwira ntchito ndi chikondi:

komatu cikhulupiriro cakucititsa mwa cikondi. (Agalatiya 5:6)

Chipatso chazimu chachikondi si chikondi ngati mmene dziko lapansi limafotokozerana. Chipatso chachikondi chenicheni ndi chikondi chopanda chinyengo. Izi zikuthauza chikondi choyera. Ichi ndi chikondi chimene mumayenera kuonetsera kwa anthu ena.

Chikondi chanu kwa Mulungu:

ndipouzikonda Ambuye Mulunguwako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse, ndi mphamvu yako yonse. (Marko 12:30)

(Werenganinso I Yohane 2:5,15; 3:11-17; 4:7-20; 5:2; II Yahane 1:5-6; Deterenome 6:5; Luke 10:27).

Tikuynera kukonda adani athu:

Koma ndinena kwa inu akumva, Kondanani nao adani anu; citirani zabwino iwo akuda inu, Ndipo 1 ngati muwakonda iwo akukondana ndinu, mudzalandira ciyamiko cotani? pakuti ocimwa omwe akonda iwo akukondana nao. Koma 3 takondanani nao adani anu, ndi kuwacitira zabwino, ndipo kongoletsani osayembekeza kanthu konse, ndipo mphotho yanu idzakhala yaikuru, ndipo 4 inu mudzakhala ana a Wamkurukuruyo; cifukwa iye acitira zokoma anthu osayamika ndi oipa. Ndipo iye ananenanso nao fanizo, 8 Kodi munthu wakhungu angathe kutsogolera mnzace wakhungu? kodi sadzagwa onse awiri m'mbuna? (Luka 6:27,32,35,39)

Munamva kuti kunanenedwa, 14 Uzikondana ndi mnansi wako, ndi kumuda mdani wako: koma Ine ndinena kwa inu, 15 Kondanani nao adani anu, ndi 16 kupempherera iwo akuzunza inu; (Mateyu 5:43-44)

Tikuyenera kukonda amzathu monga tidzikondera ife mwini:

Lemekeza atate wako ndi amako, ndipo, Uzikonda mnzako monga udzikonda iwe mwini. (Mateyu 19:19)

Yesu akufuna kuti ife tikonde ngati mmene Iye anatikondera ife:

Monga momwe Atate wandikonda Ine, Inenso ndakonda inu; khalani m'cikondi canga. Lamulo langa ndi ili, kuti mukondane wina ndi mnzace, monga ndakonda inu. (Yohane 15:9,12)

ndipo ndinazindikiritsa iwo dzina lanu, ndipo ndidzalizindikiritsa; kuti cikondi 7 cimene munandikonda naco cikhale mwa iwo, ndi Ine mwa iwo. (Yohane 17:26)

Ndio kudzera muchikondano cha wina ndi mzake chimene anthu angadziwire kuti ndife akhristu.

Yohane 13:35 1 Mwa ici adzazindikira onse kuti muli akuphunzira anga, ngati muli naco cikondano wina ndi mnzace. (John 13:35)

Ngati sitimakonda okhukupirira ena, chikondi cha Mulungu chimakhala kuti sichili paife.

iyе amene anena kuti ali m'kuunika, namuda mbale wace, ali mundima kufikira tsopane lino. Iye amene akonda mbale wace akhala m'kuunika, ndipo mwa iye mulibe cokhumudwitsa. (Yohane 2:9-10).

(Ichi ndi choonadi champhamvu ndi chachikulu. Werengani zambiri zachikondi mu buku la Yohane 13:34; 14:15,21,23,31; 15:9-19; 17:26;21:15-17).

Chikondi chatu chikuyenera kukula:

Ndipo ici ndipempha, kuti cikondi canu cisefukire cionjezere, m'cidziwitso, ndi kuzindikira konse; (Afilipi 1:9)

koma Ambuye akukulitseni inu, nakueurukitseni m'cikondano wina kwa mnzace ndi kwa anthu onse, monganso ife titero kwa inu;(1 Atesalonika 3:12)

Tikuyenera kukhazikika ndikuzikika pachikondi:

kuti Kristu akhale cikhali mwa cikhulupiriro m'mitima yanu; kuti, ozika mizu ndi otsendereka m'cikondi, mukakhozetu kuzindikira pamodzi ndi oyera mtima onse, kupingasa, ndi utali, ndi kukwera, ndi kuzama nciani; ndi kuzindikira cikondi ca Kristu, cakuposa mazindikiridwe, kuti mukadzazidwe kufikira cidzalo conse ca Mulungu. (Aefeso 3:17-19)

Mukuyenera kubala kapena kukhala ndi ena mwachikondi:

ndi kuonetsera kudzicepetsa konse, ndi cifatso, ndi kuonetsera cipiriro, ndi kulolerana wina ndi mnzace, mwa cikondi; (Aefeso 4:2)

Mukuyenera kukhalabe muchikondi:

mudzisunge nokha m'cikondi ca Mulungu, (Yuda 1:21)

Koma iwe, munthu wa Mulungu iwe, thawa izi; nutsate cilungamo, cipembedzo, cikhulupiriro, cikondi, cipiriro, cifatso. (1 Timoteo 6:11)

Kugwira ntchito kwanu mwa Mulungu kukuyenera kukhala chikondi:

ndi kukumbukila kosalekeza nchito yanu ya cikhulupiriro, ndi cikondi (1 Atesalonika 1:3)

pakuti Mulungusali wosalungama kuti adzaiwala nchito yanu, ndi cikondico mudacionetsera ku dzina lace, umo mudatumikira oyera mtima ndi kuwatumikirabe. (Ahebri 6:10)

Pamene chimalizira chidzatsala pang'ono, chikondano cha anthu ambiri chidzazilara. Izi zikutanthauza kuti anthu adzakhalao osasamala za anthu ena.

Ndipo cifukwa ca kucuruka kwa kusayeruzika, cikondano ca anthu aunyinji cidzazirala. (Mateyu 24:12)

Koma tinapatsidwa chitsikimizo kuti palibe chidzatilekanitse ndi chikondi cha Mulungu:

Adzatisiyanitsa ndani ndi cikondi ca Kristu? nsautso kodi, kapena kupsinjika mtima, kapena kuzunza, kapena njala, kapena usiwa, kapena zoopsy kapena lupanga kodi? Pakuti ndakopeka mtima kuti ngakhale imfa, ngakhale moyo, ngakhale angelo, ngakhale maufumu, ngakhale zinthu ziripo, ngakhale zinthu zirinkudza, ngakhale zimphamvu, ngakhale utali, ngakhale kuya, ngakhale colengedwa cina ciri conse, sicingadzakhoze kutisiyanitsa ife ndi cikondi ca Mulungu, cimene ciri mwa Kristu Yesu Ambuye wathu. (Aroma 8:35,38-39)

Davide analemba zambir zokhudza chikondi. Werengani Salimo 31:23; 18:1; 40:16; 97:10; 116:1; 119:97, 113, 119,127, 132, 159, 163, 105, 167; 122:6; 145:20. Werenganinso buku la 1 Yohane limene mutu wake umodzi umene ndi waukulu ndi chikondi.

CHIMWEMWE

Chimwemwe ndi kukondwelera, kapena kukhala okondwa.

Mphatso ya chimwemwe ndi kusangalala ndi zinthu zosiyana. Zinthu ziwirizi zimachoka malo osiyana. Chisangalalo chimachoka pa zinthu zimene zakuzungulirani komanso chimatengera nyengo zimene mukudutsamo. Chimwemwe chimachokera kwa Mzimu wa Mulungu ndipo sichitengera zimene mukudutsamo:

Yesu Khristu anabweleretsa chimwemwe chifukwa chakubadwa kwake:

Ndipo mngelo anati kwa iwo, Musaope; pakuti onani, ndikuuzani inu uthenga wabwino wa cikondwero cacikuru, cimene cidzakhala kwa anthu onse; pakuti wakubadwirani inu lero, m'mudzi wa Davide, Mpulumutsi, amene ali Kristu Ambuye. (Luka 2:10-11)

Ndichifuniro cha Mulungu kuti mukhale ndi chimwemwe:

Izi ndalankhula ndi inu, kuti cimwemwe canga cikhale mwa inu, ndi kuti cimwemwe canu cidzale. (Yohane 15:11)

Koma tso pane ndidza kwa Inu; ndipo izi ndilankhula m'dziko lapansi, kuti akhale naco cimwemwe canga cokwaniridwa mwa iwo okha. (Yohane 17:13)

Ophunzira a Yesu anadzadzidwa ndi chimwemwe atalandira Mzimu Woyera:

Ndipo akuphunzira anadzazidwa ndi cimwemwe ndi Mzimu Woyera . (Macitidwe)

Gwero la chimwemwe cha anthu okhulupirira si zinthu zakudziko koma Mulungu:

Pankhope panu pali cimwemwe cokwanira; M'dzanja lanu lamanja muli zokondweretsa zomka muyaya. (Masalmo 16:11)

Chifukwa chakuti chimwemwe ndi chinthu chauzimu chimene sichitemgera nyengo zanu zakuthupi, mukhoza kukondwerabe ngakhale muchiyero:

Muciyese cimwemwe cokha, abale anga, m'mene mukugwa m'mayesero a mitundu mitundu; (Yakobo 1:2)

Mukhoza kukondwera ngakhale munyengo zowawa kapena chizunzo chimene”

**ndidzazidwa naco citonthozo, ndisefukira naco cimwemwe m'cisautso cathu conse.
(2 Akorinto 7:4)**

Mukhoza kumazuzika koma ndi chimwemwe:

**olimbikitsidwa m'cilimbiko conse, monga mwa mphamvu ya ulemerero wace,
kucitira cipiriro conse ndi kuleza mtima conse pamodzi ndi cimwemwe, (Akolose
1:11)**

Chimwemwe ndi mbali imodzi ya Ufumu wa Mulungu:

**Pakuti ufumu wa Mulungusukhala cakudya ndi cakumwa, koma cilungamo, ndi
mtendere, ndi cimwemwe mwa Mzimu Woyera . (Aroma 14:17)**

Baibulo limalimbikitsa okhulupirira kuti ayenera kuonetsera chimwemwe chao mwa Mulungu:

**Koma akondwere onse amene athawira kwa Inu, Apfuule mokondwera kosaleka,
popeza muwafungatira; Nasekere mwa Inu iwo akukonda dzina lanu. (Masalmo
5:11)**

(Werengani Salimo 35:9; 63:5; 66:1; 81:1; 95:1-2; 149:5; 98:4,6,8; 100:1).

MTENDERE

Mtendere ndi pamene palibe kulimbana, nkhawa komanso ndi pamene pali bata ndi kuyanjana. Mtendera sikukhala chete osachita kenakalikonse ayi. Nthawi zina mtendera umabwera chifukwa chogwiritsa ntchito mphamvu monga mmene asungitsa bata amachitira.

Chisokonezo ndi mau otsutsana ndi mau oti mtendere. Mulungu samabweretsa chisokonezo. Cholinga chake ndi ndikubweretsa mtendera:

**pakuti Mulungusali Mulunguwa cisokonezo koma wa mtendere; monga mwa
Mipingo yonse ya oyera mtima (1 Akorinto 14:33)**

Yesu Khristu anabweretsa mtendere pa dziko lapansi:

**pakuti Mulungusali Mulunguwa cisokonezo koma wa mtendere; monga mwa
Mipingo yonse ya oyera mtima. (1 Akorinto 14:33)**

Mtendere weniweni umachokera mwa Yesu:

**Mau amene anatumiza kwa ana a Israyeli, akulalikira Uthenga Wabwino wa
mtendere mwa Yesu Kristu (ndiye Ambuye wa onse) ... (Macitidwe 10:36)**

**Pakuti iye ndiye mtendere wathu, amene anacita kutionse awiri akhale mmodzi,
nagumula khoma lakudulitsa pakati, (Aefeso 2:14)**

**Popeza tsono tayesedwa olungama ndi cikhulupiriro, tikhala ndi mtendere ndi
Mulungumwa Ambuye wathu Yesu Kristu; (Aroma 5:1)**

Yesu Khristu anasiyira ophunzira ake mtendera wake wapadera:

Zinthu izi ndalankhula ndi inu, kuti mwa Ine mukakhale nao mtendere. M'dziko lapansi mudzakhala naco cibvuto, koma limbikani mtima; ndalilaka dziko lapansi Ine. (Yohane 16:33)

Uthenga Wabwino ndi wamtendere:

ndipo mutadzibveka mapazi anu ndi makonzedwe a Uthenga Wabwino wa mtendere; (Aefeso 6:15)

Pali mitundu iwiri ya mtendere: Mtendere oyamaba ndi mtendere ndi Mulungu:

Popeza tsono tayesedwa olungama ndi cikhulupiriro, tikhala ndi mtendere ndi Mulungumwa Ambuye wathu Yesu Kristu; (Aroma 5:1)

Pamene mwakhazikitsa mtendere ndi Mulungu, mukhoza kukhala ndi mtendere wa Mulungu mmoyo wanu:

Ndipo mtendere wa Mulunguwakupambana cidziwitso conse, udzasunga mitima yanu ndi maganizo anu mwa Kristu Yesu. (Afilipi 4:7)

Tikuzidwa kuti tikuyenera kutsata zinthu zimene zikhoza kubweretsa mtendere:

Cifukwa cace tilondole zinthu za mtendere, ndi zinthu zakulimbikitsana wina ndi mnzace. (Aroma 14:19)

Tiyenera kukhala mumtendere:

Cotsalira, abale, kondwerani, Mucitidwe angwiro; mutorithozedwe; khalani a mtima umodzi, khalani mumtendere; ndipo Mulunguwa cikondi ndi mtendere akhale pamodzi ndi inu. (2 Akorinto 13:11)

Tiyenera kusunga umodzi kudzera mu Mzimu Woyera:

Tikuyenera kukhala mumtendere ndi anthu onse:

Londolani mtendere ndi anthu onse: (Ahebri 12:14)

Tikuyenera kusunga umodzi wa Mzimu kudzera mu mtendere.

ndi kusamalitsa kusunga umodzi wa Mzimu mwa cimangiriro ca mtendere. (Aefeso 4:3)

Mtendere wa Mulungu ukuyenera kulamulira mitima yathu:

Tonsefe amene tsono tidakonzeka amphumphu, tilingirire ici mumtima; ndipo ngati kuli kanthu mulingirira nako kwina mumtima, akanso Mulunguadzabvumbulutsira inu; (Afilipi 3:15)

Tikuyenera kukhala pamtendera nthawi zonse:

kuti mupezedwe ndi iye mmtendere, (2 Petro 3:14)

CHIPIRIRO/KULEKELERA

Kulekelera kapena chipiriro ndi kukhala ndi kudekha kapena ndi kuthekera kotha kudutsa munyengo zowawa ndi kuzipirira. Kulekelera kapena chipiriro ndi chikhalidwe cha Mulungu.

Ndipo Yehova anapita pamaso pace, napfuula, Yehova, Yehova, Mulunguwacifundo ndi wacisomo, wolekereza, ndi wa ukoma mtima wocuruka, ndi wacoonadi; (Eksodo 34:6)

Yehova ndiye wolekereza, ndi wa cifundo cocuruka, wokhulukira mphulupulu ndi kulakwa, koma wosamasula woparamula; wakuwalanga ana cifukwa ca mphulupulu ya atate ao, kufikira mbadwo wacitatu ndi wacinai. (Numeri 14:18)

Koma Inu, Ambuye, ndinu Mulunguwasoni ndi wacisomo, Wosapsa mtima msanga, ndi wocurukira cifundo ndi coonadi. (Masalmo 86:15)

Ndipo yesani kulekerera kwa Ambuye wathu cipulumutso; monganso mbale wathu wokonedwa Paulo, monga mwa nzeru zopatsidwa cwa iye, anakulemberani; (2 Petro 3:15)

Kapena upeputsa kodi kulemera kwa ubwino wace, ndi cilekerero ndi cipiriro cace, wosadziwa kuti ubwino wa Mulunguukubwezera kuti ulape? (Aroma 2:4)

Chipiriro chinali chinthu chimodzi chimene chimaonekera mu utumiki wa Mtumwi Paulo:

Koma iwe watsatatsata ciphunzitso canga, mayendedwe, citsimikizo mtima, cikhulupiriro, kuleza mtima, cikondi, cipiriro, (2 Timoteo 3:10)

Timauzidwa kuti tikuyenera kukhala ndi chipiriro komanso okondwera.

olimbikitsidwa m'cilimbiko conse, monga mwa mphamvu ya ulemerero wace, kucitira cipiriro conse ndi kuleza mtima conse pamodzi ndi cimwemwe, (Akolose 1:11)

Tikuyenera kukhala opirira:

ndi kuonetsera kudzicepetsa conse, ndi cifatso, ndi kuonetsera cipiriro, ndi kulolerana wina ndi mnzace, mwa cikondi; (Aefeso 4:2)

Tikuyenera kulalika mau a Mulungu ndi chipiriro:

lalikira mau; cita nao pa nthawi yace, popanda nthawi yace; tsutsa, dzudzula, cenjeza, ndi kuleza mtima conse ndi ciphunzitso. (Timoteo 4:2)

Okhulupirira ayenera kukhala ndi chipiriro ngati chikhalidwe chauzimu.

Cifukwa cace bvalani, monga osankhika a Mulungu, oyera mtima ndi okonedwa, mtima wacifundo, kukoma mtima, kudzicepetsa, cifatso, kuleza mtima: (Akolose 3:12)

KULEZA

Kuleza ndi khalidwe lotha kudziletsa, kapena kuti kusakhala munthu wandeu. Kuzela ndi kukhala ndi chifundo.

Ndipo kapolo wa Ambuye sayenera kucita ndeu, komatu akhale woyenera, waulere pa onse, wodziwa kuphunzitsa, woleza, (2 Timoteo 2:24)

Baibulo limachenjeza okhulupilira kuti sayenera kukhala a ndeu koma ayenera kukhala woleza:

Ndipo kapolo wa Ambuye sayenera kucita ndeu, komatu akhale woyenera, waulere pa onse, wodziwa kuphunzitsa, woleza, (2 Timoteo 2:24)

Sitikuyenera kukhala anthu andeu. Anthu andeu ndi anthu amene amakhala akufuna kumenya kapena kulimbana ndi anthu ena.

asacitire mwano munthu ali yense, asakhale andeu, akhale aulere, naonetsere cifatso conse pa anthu onse. (Tito 3:2)

Chifukwa cha kuleza, tikuyenera kukhala anthu ofikilika andi anthu ena:

Koma nzeru yocokera kumwamba iyamba kukhala yoyera, nikhalanso yamtendere, yaulere, yomvera bwino, yodzala cifundo ndi zipatso zabwino, yopanda tsankhu, yosadzikometsera pamaso. (Yakobo 3:17)

Davite anati:

Ndipo mwandipatsa cikopa ca cipulumutso canu: Ndipo dzanja lamanja lanu landigwiriziza, Ndipo cifatso canu candikuza ine. (Masalmo 18:35)

CHIFUNDO

Chifundo ndi ugwiro kapena chiyero cha Mulungu. Chifundo ndi chikhalidwe cha Mulungu.

Ciweruzo ca Yehova cikhazikika cikhazikikire, Zolingirira za m'mtima mwace ku mibadwo mibadwo. (Masalmo 33:11)

**Ayamike Yehova cifukwa ca cifundo cace, Ndi zodabwiza zace za kwa ana a anthu!
Ayamike Yehova cifukwa ca cifundo cace, Ndi zodabwiza zace za kwa ana a anthu!
Ayamike Yehova cifukwa ca cifundo cace, Ndi zodabwiza zace za kwa ana a anthu!
Ayamike Yehova cifukwa ca cifundo cace, Ndi zodabwiza zace za kwa ana a anthu!
(Masalmo 107:8,15,21,31)**

**Ndiye cifundo canga, ndi linga langa, Msanje wanga, ndi mpulumutsi wanga;
Cikopa canga, ndi Iye amene ndimtima; Amene andigonjetsera anthu anga.
(Masalmo 144:2)**

Ngakhale dziko lapansi limaonetsera chifundo cha Mulungu:

... Dziko lapansi ladzala ndi cifundo ca Yehova. (Masalmo 33:5)

Madalitso onse a chaka chonse amachokera kwa Mulungu:

Mubveka cakaci ndi kukoma wanu; (Masalmo 65:11)

Chifundo cha Mulungu chimaonekera pa anthu ochimwa pamene Mulungu awatsogolera kuti alape:

Pakuti dzina la Mulungu lilitidwa mwano cifukwa ca inu, pakati pa anthu a mitundu, monga mwalembedwa.? (Aroma 2:24)

Mfumu Davite ikufotokoza kuti pachipanda Yehova kukhulupilira ubwino wa Mulungu akanasowa pogwira:

Ndikadapanda kukhulupirira kuti ndikaone ubwino wa Yehova M'dziko la amoyo, ndikadatanil. (Masalmo 27:13)

Ha! kukoma kwanu ndiko kwakukuru nanga, kumene munasungira iwo akuopa Inu, Kumene munacitira iwo akukhulupirira Inu, pamaso pa ana a anthu! (Masalmo 31:19)

Mulungu akhutitsa anthu onse akulakalaka:

Pakuti akhutitsa mtima wolakalaka, Nadzaza mtima wanjala ndi zabwino. (Masalmo 107:9)

Ngati okhulupirira chifundo ndi ubwino wa Mulungu umatitsata:

Inde ukoma ndi cifundo zidzanditsata masiku onse a moyo wanga: Ndipo ndidzakhala m'nyumba ya Yehova masiku onse. (Masalmo 23:6)

CHIKHULUPIRIRO

Mwaphunzira kale za chikhulupiriro ngati mphatso imodzi yauzimu. Zinthu zimene zinaphunzitsidwa zokhudza chikhulupiriro ngati mphatso zimagwirizananso ndi chikhulupiriro ngati chipatso cha Mzimu Woyera.

Komabe mukuyenera kukumbukira kusiyana pakati pa zinthu ziwirizi kumene kunavotokozeredwa kale kuja. Chikhulupiriro ngati mphatso ndi mphamvu ya Mulungu. Ndi chikhulupiriro cha mphamvu ya Mulungu mukhoza kuchita kanthu kamene anthu ena sangathe kuchita chifukwa chopanda chikhulupiriro. Chikhulupiriro ndi chipatso cha khalidwe. Ndichikhazikitso chokhala ndi chikhulupiriro ndi Mulungu. Ngakhale kuti wina aliyense sangakhale ndi mphatso ya chikhulupiro, chipatso chachikhulupiriro Chikuyenera kuoneka mwa okhulupirira wina aliyense.

CHIFATSO

Kufatsa ndi kukhala ndikudziletsa pogwiritsa ntchito mphamvu. Chifatso ndi njira imene imagwira ntchito yomukonza munthu amene wabwelerera pamaso pa Mulungu. Munthu wakugwa ndi munthu amene wabweleranso kumachimo ake atalandira Yesu Khristu ngati mbuye ndi mpulumutsi.

Cifukwa cace bvalani, monga osankhika a Mulungu, oyera mtima ndi okondedwa, mtima wacifundo, kukoma mtima, kudzicepetsa, cifatso, kuleza mtima; kulolerana wina ndi mnzace, ndi kukhululukirana eni okha, ngati wina ali naco cifukwa pa mnzace; monganso Ambuye anakhululukira inu, teroni inunso; (Akolose 3:12-13)

Abale, ngatinso munthu agwidwa nako kulakwa kwakuti, inu auzimu, mubweze wotereyo mu mzimu wa cifatso; ndikudzipenyenera wekha, ungayesedwe nawenso. (Agalatiya 6:1)

Chifatso chimathandiza kusunga umodzi mumpingo:

Ndikudandaulirani inu tsono, ine wandende mwa Ambuye, muyende koyenera maitanidwe amene munaitanidwa nao, ndi kuonetsera kudzicepetsa konse, ndi cifatso, ndi kuonetsera cipiriro, ndi kulolerana wina ndi mnzace, mwa cikondi; ndi kusamalitsa kusunga umodzi wa Mzimu mwa cimangiriro ca mtendere. (Aefeso 4:1-3)

Chifatso chiyenera kugwiritsidwa ntchito potsogolera anthu.

Ndipo kapolo wa Ambuye sayenera kucita ndeu, komatu akhale woyenera, waulere pa onse, wodziwa kuphunzitsa, woleza, 1 wolangiza iwo akutsutsana mofatsa; 2 ngati kapena Mulunguawapatse iwo citembenuziro, kukazindikira coonadi, (2 Timoteo 2:24-25)

asacitire mwano munthu ali yense, asakhale andeu, akhale aulere, naonetsere cifatso conse pa anthu onse. Tito 3:2)

Tikuyenera kulandira mau a Mulungu ndi chifatso:

Mwa ici, mutabvula cinyanso conse ndi cifukiro ca coipa, landirani ndi cifatso mau ookedwa mwa inu, okhoza kupulumutsa moyo wanu. (Yakobo 1:21)

Munthu wanzeru amakhala wofatsa:

Ndani ali wanzeru, ndi waluso mwa inu? Aonetsere ndi mayendedwe ace abwino nchito zace mu nzeru yofatsa. (Yakobo 3:13)

Tikukulimbikitsidwa ngati okhulupirira kufunafuna chifatso:

Cifukwa cace bvalani, monga osankhika a Mulungu, oyera mtima ndi okondedwa, mtima wacifundo, kukoma mtima, kudzicepetsa, cifatso, kuleza mtima; Akolose 3:12)

Koma iwe, munthu wa Mulunguiwe, thawa izi; nutsate cilungamo, cipembedzo, cikhulupiriro, cikondi, cipiriro, cifatso. (1 Timoteo 6:11)

Koma iwe, munthu wa Mulunguiwe, thawa izi; nutsate cilungamo, cipembedzo, cikhulupiriro, cikondi, cipiriro, cifatso. (1 Timoteo 6:11)

KUDZILETSA

Kudziletsa ndi kudzibwenza mumaganizidwe kapena muzochita zathu. Kudziletsa ndi chinsisi cha zonse.

koma 4 ndipumpuatha thupi langa, ndipo ndiliyesa capolo; kuti, kapena ngakhale rdalalikira kwa ena, 5 ndingakhale votayika ndekha. (1 Akorinto 9:27).

Baibulo limafotokoza kitu tikuyenera kukhaka odziletsa mmoyo wathu:

ndi pacodziletsa cipiriro; (2 Petro 1:6)

Kudziletsa kunali gawo limodzi la Uthenga Wabwino wa Paulo.

Ndipo m'mene anamfotokozerwa za cilungamo, ndi cidziletso, (Macitidwe 24:25)

KUFUNIKA KWA CHIPATSO

Yesu anatsindika kwambiri zakubala chipatso. Mufanizo lake lina iye anati:

Ndipo iye ananena fanizo ili: Munthu wina anali ndi mkuyu wookam'munda wace wamphesa. Ndipo anadza nafuna cipatso pa uwu, koma anapeza palibe. Ndipo anati kwa wosungira munda wamphesa, Taona, zaka zapita zitatu ndimadza ine kudzafuna cipatso pa mkuyu uwu, ndipo ndimapeza palibe: taulikha; uyeseranjinso nthaka yopanda pace? Ndipo iye anayankha nanena naye, Mbuye, baulekani ngakhale caka cino comwe, kufikira ndidzaukumbira kwete, ndithirepo ndowe; ndipo, ngati udzabala cipatso kuyambira pamenepo, cabwino; koma ngati iai, mudza ulikhatu. (Luka 13:6-9)

(Luke 13:6-9)

Yesu ataona mtengo wamkhuyu opanda chipatso anati:

Ndipo mamawa, m'mene Iye analinkunkanso kumzinda, anamva njala, Ndipo pakuona mkuyu umodzi panjira, anafika pamenepo, napeza palibe kanthu koma masamba okha okha; nati Iye kwa uwo, Sudzabalanso cipatso ku nthawi zonse. Ndipo pomwepo mkuyuwo unafota. (Mateyu 21:18-19)

Sikuti Yesu anatembelera mtengo uja chifukwa cha njala ndipo kuti mtengowo unalibe chipatso. Iye amatsindika kapena kuphunzitsa za choonadi chofunika kwambiri. Mtengo wamkhuyu unali ndi maonekedwa abwino kwambiri, unali obiriwira bwino kwambiri kotero kuti umaoneka ngati ukhoza kukhala ndi zipatso. Koma mtengou unalibe chipatso chinachilichonse.

Mulungu amakhudzika ndi kubala chipatso osati kungokhala ndi maonekedwa okhala ngati pali zipatso.

Pakhala kutsindika kwa kukulu kwa mpato za Mzimu Woyera kusiyana ndi chipatso cha Mzimu Woyera mu mautumiki ambiro a lero lino. Koma Baibulo limatsindika kwambiri za Chipatso cha Mzimu Woyera.

Inde comweco pa zipatso zao mudzawazindikira iwo. (Mateyu 7:20)

Chipatso chimene munthu amaonetsa chimaonetsera chimene chili mkati mwakwe:

Pakuti 11 palibe mtengo wabwino wakupatsa zipatso zobvunda; kapenanso mtengo woipa wakupatsa zipatso zabwino, Pakuti mtengo uli wonse uzindikirika ndi cipatso cace. Pakuti anthu samachera nkhuju paminga, kapena pamtungwi samachera mphesa, Munthu wabwino aturutsa zabwino m'cuma cokoma ca mtima wace; ndi munthu woipa aturutsa zoipa m'coipa cace: pakuti m'kamwa mwace mungolankhula mwa kukuruka kwa mtima wace. (Luka 6:43-45)

Munthu akhoza kukhala ndi chikoka chakunja, koma izi sizitanthauza kuti iye ali ndi mpamvu yauzimu. Ndipo iye akhoza kuchita zodabwino mudzina la Mulungu, koma Yesu anati:

Si yense wakunena kwa Ine, Ambuye, Ambuye, adzalowa mu Ufumu wa Kumwamba; koma wakucitayo cifuniro ca Atate wanga wa Kumwamba. Ambiri adzati kwa Ine tsiku lomwelo, Ambuye, Ambuye, kodi sitinanenera mau m'dzina lanu, ndi m'dzina lanunso kuturutsa mizimu yoipa, ndi kucita m'dzina lanunso zamphamvu zambiri? Ndipo pamenepo ndidzafukulira iwo, Sindinakudziwani inu nthawi zonse; cokani kwa Ine, inu akucita kusayeruzika. (Mateyu 7:21-23)

Yuda akuchenjeza za anthu amene adzalowa mu mpingo wa ambuye ndi kuyamba kuphunzitsa chiphunzitsa chonyenga. Iye akufotokoza kuti njira imodzo yozindikira anthu amenewa ndi yakuti amakhala opanda chipatso cha Mzimu Woyera mmoyo wao.

Iwo ndiwo okhala mawanga pa mapwando anu a cikondano, pakudya nanu pamodzi, akudziweta okha opanda mantha; mitambo yopanda madzi, yotengekatengeka ndi mphepo; mitengo ya masika yopanda zipatso, yofafa kawid, yozuka mizu; (Yuda 1:12)

Chinthu chofunika kwambiri muutumiki ndi chipatso. ... **“Ndi ZIPATSO zawo mudzawadziwa”** (Mateyu 7:20)

Kudziko lakuthupi, chipatso ndi chimene chimanyamula njera zimene zimatha kubalanso. Pamene mu dziko lauzimu, ndi Mzimu Woyera amene ali ndi kuthekera kotithandiza kuti tibale zipatso:

- Chipatso cha khalidwe longa ngati la Yesu limakopa anthu ochimwa kwa Yesu.
- Chipatso cha mlaliki chimafalitsa uthenga wa Ufumu wa Mulungu ndipo zotsatira zake ndi kholora lauzimu pa dziko lonse lapansi.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Kodi chipatso chazimu ndi chiani?

2. Kodi chipatso chamkati cha Mzimu ndi chiani?

3. Tchulani makhalidwe a chipatso chamkati cha Mzimu Woyera.

_____	_____
_____	_____
_____	_____
_____	_____
_____	_____

4. Kodi ndi umboni uti opezeka m'baibulo umene umaonetsa kuti Yesu anatisankha kuti tibale chipatso?

5. Lembani vesi yotsogolera osaonera

6. Werengani mndandanda wa chipatso chazimu cha Mzimu Woyera mu gawo 1. Ndipo werenganinso mndandanda 2 umene uli ndi matanthauzo a mpatso zimene zaperekedwe mu gawo 1. Lembani nambala pampata waperekedwawo imene ikufotokoza tanthauzo lachipatso.

- | | |
|--------------------|---|
| ___ Kudziletsa | 1. Chikondi chozama komanso kusamala anthu ena. |
| ___ Chikhulupiriro | 2. Kukondwera kapena kusangalala. |
| ___ Chifatso | 3. Kukhala wachete, odekha komanso wantendere. |
| ___ Kuleza | 4. Kupirira |
| ___ Chifundo | 5. Kudziletsa kapena kudzibweza. |
| ___ Chimwemwe | 6. Ntchito zangwiro. |
| ___ Chipiriro | 7. Chikhulupiriro cha mpamvu mwa Mulungu. |
| ___ Mtendera | 8. Kudzibweza pogwiritsa ntchito mphamvu. |

___ Chikondi

9. Kudzibweza wekha kapena kudziletsa

7. Kodi chipatso cha Mzimu ndi chofunika bwanji?

8. Kodi pali kusiyana bwanji pakati pa mtendere ndi Mulungu ndi mtendere wa Mulungu.

(mayankho amafunsowa ali kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Werengani Mateyu 5:1-12. Kodi ndi zipatso zingati za khalidwe longa la Yesu tikupeza mu ndime imeneyi. Mwachitsanzo, chipatso cha chimwemwe chikutchulidwa pa vesi 12.
2. Werengani I Akorinto chaputala 13 pamene akukamba zambiri zokhudza chipatso chachikondi. Kodi ndi zipatso zina zingati zimene zikuonekera kudzera muchikondi? Mwachitsanzo, vesi 7 ikuonetsera za chipatso cha chikhulupiriro.
3. Chipatso chauzimu chimaonetsera chikhalidwe cha Mulungu. Mulungu ali ndi:

Chimwemwe: Mateyu 25:21

Mtendere: Afilipo 4:7

Chipiriro: II Petro 3:9,15

Kuleza: Mateyu 11:28-30

Ubwino: II Petro 1:3

Kukhulupirika: II Timoteo 2:13

Chifatso: Zefaniya 2:3

Kidzoletsa: Ahebri 12:11 (Chilango cha Mulunguchofuna kukonza).

4. Moyo wa Yesu Khristu amaonetsera chipatso chinachilichonse:

Chipatso chakunja: Kulalikira: Yohane 10:16; Marko 1:38.

Chipatso chamkati:

Chikondi: Marko 10:21; Yohane 11:5,36

Chimwemwe: Yohane 15:11

Mtendere: Yohane 14:27

Chipiriro: I Petro 3:15

Kuleza: II Akorinto 10:1

Ubwino: Aroma 11:22

Kukhulupirika: Mateyu 17:14-21

Chifatso: Luka 4:1-13

Werengani mabuku a Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane. Ndipo onjezera ma vesi ena amene Yesu anaonetsera chipatso cha Mzimu Woyera.

CHAPUTALA 12

NTCHITO ZAKUTHUPI

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziri ili muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kuzindikira ntchito zakuthupi.
- Kufotokoza mmene mungayendera mumzimu osati kuthupi.

VESI YOTSOGOLERA.

Ndipo nchito za thupi zionekera, ndizo dama, codetsa, kukhumba zonyansa, kupembedza mafano, nyanga, madano, ndeu, kaduka, zopsa mtima, zotetana, magawano, mipatuko, njiru, kuledzera, mcezo, ndi zina zotere; zimene ndikucenjezani nazo, monga ndacita, kuti iwo akucitacita zotere sadzalowa Ufumu wa Mulungu. (Agalatiya 5:19-21)

CHIYAMBI

Chaputala ichi chikhazika pa ntchito zakuthupi, izi ndi ntchito zauchimo zimene zimakhala zosemphana ndi chipatsa cha Mzimu Woyera.

KODI NTCHITO ZAKUTHUPI NDI CHIANI?

Ntchito zakuthupi ndi chikhalidwe chimene munthu ochimwa amaonetsera chifukwa chazilakolako cha chauzimu. Ichi ndi chikhalidwe chimene chimakhala chosemphana ndi chikhalidwe chimene Mzimu Woyera amafuna kukuza mmoyo wa munthu okhulupirira.

NKHONDO YAUZIMU

Pali nkondo yauzimu imene imakhala ikumenenyedwa mmoyo wa munthu okhulupirira. Ntchito zauzimu zakuthupi cholinga chake ndikuononga chipatso cha Mzimu Woyera.

Pakuti thupi lilakalaka potsutsana naye Mzimu, ndi Mzimu potsutsana nalo thupi; pakuti izi sizilingana; kuti zimene muzifuna musazicite. (Agalatiya 5:17)

Zilakolako zakuthupi za munthu ndi zosemphani ndi chikhalidwe cha Mzimu Woyera.

Ntchito zathupi ndi:

Ndipo nchito za thupi zionekera, ndizo dama, codetsa, kukhumba zonyansa, kupembedza mafano, nyanga, madano, ndeu, kaduka, zopsa mtima, zotetana, magawano, mipatuko, njiru, kuledzera, mcezo, ndi zina zotere; zimene ndikucenjezani nazo, monga ndacita, kuti iwo akucitacita zotere sadzalowa Ufumu wa Mulungu. (Agalatiya 5:19-21)

Zotsatira zamachimo amenewa zimaonekera mu zinthu zolakwika, ngakhale kuti chiyambi chake ndi chilakolako chauchimo.

Ndipo ananena nao, Mutero inunso opanda nzeru kodi? Kodi simuzindikira kuti kanthu kali konse kocokera kunja kakulowa mwa munthu, sikangathe kumdetsa iye; Ndipo anati, Coturuka mwa munthu ndico cidetsa munthu. zoipa izi zonse zituruka m'kati, nizidetsa munthu. (Marko 7:18,20,23)

Machimo amene atchulidwa pa Agalatiya 5:19-21 simachimo okhao amene Baibulo limatchula. Pali gulu lina lamachimo amene amatchedwa “ntchito zakuthupi” zimene zimakhala zotsutsana ndi chipatso cha Mzimu Woyera. Ichi ndi chifukwa chake tikufuna kuphunzira mwapadera machimo amenewa.

CHIGOLORO

Chigolora ndi mtchitidwe ogonana pakati pa munthu okwatira ndi munthu wina amene si mkazi wao. Limodzi mwa malamuro khumi a Mulungundi lakuti:

Usacite cigololo. (Eksodo 20:14)

Munthawi ya Chipangano chakale, Munthu amene amapezeka attachita chigoloro amaphedwa poponyedwa miyala:

Munthu akacita cigololo ndi mkazi wa mwini, popeza wacita cigololo ndi mkazi wa mnansi wace, awaphe nditho, mwamuna ndi mkazi onse awiri. (Levitiko 20:10)

Malingana ndi Yesu Khristu, maganizo ena aliwonse onyansa okhudza kugonana akhoza ndi chigoloro:

Munamva kuti kunanenedwa, Usacite cigololo; koma Ine ndinena kwa inu, kuti yense wakuyang'ana mkazi kumkhumba, pamenepo watha kucita naye cigololo mumtima mwace. (Mateyu 5:27-28)

Kusiya mkazi wako kapena mamuna wako popanda chifukwa chogwirizana ndi Baibulo ndi Baibulo ndi chigoloro:

koma Ine ndinena kwa inu, kuti 4 yense wakucotsa mkazi wace, kosati cifukwa ca cigololo, amcititsa cigololo: ndipo amene adzakwata wocotsedwayo acita cigololo. (Mateyu 5:32)

ndipo ngati mkazi akacotsa mwamuna wace, nakwatiwa ndi wina, acita cigololo iyeyu. (Marko 10:12)

Munthu amene amachita chigoloro amakhala kuti akuchimwila moyo wake omwe:

Wocita cigololo ndi mkazi alibe nzeru; Wofuna kuononga moyo wace wace ndiye amatero. (Miyambi 6:32)

Chiweruzo cha Mulungu chiri paonse akuchita chigoloro:

Ukwati ucitidwe ulemu ndi onse, ndi pogona pakhale posadetsedwa; pakuti adama ndi acigololo adzawaweruza Mulungu. (Ahebri 13:4)

Onse achita chigoloro sakalowa Ufumu wakumwamba:

**Kapenasimudziwa kuti osalungama sadzalandira ufumu wa Mulungu?
Musasoceretsedwe; adama, kapena opembedza mafano, kapena acigololo, kapena olobodoka ndi zoipa, kapena akudziipsa ndi amuna, (I Akorinto 6:9)**

Chizindikiro chimodzi chimene mukhoza kuzindikira nacho aphunzitsi onyenga ndi tchimo la chigoloro.

... Koma padakhalanso pakati pa anthuwo aneneri onama, monganso padzakhala aphunzitsi onama pakati pa inu, amene adzalowa nayo m'tseri mipatuko yotayikitsa, nadzakana Ambuye amene adawagula, nadzadzitengera iwo okha citayiko cakudza msanga. okhala nao maso odzala ndi cigololo, osakhoza kuleka ucimo, kunyengerera iwo a moyo wosakhazikika; okhala nao mtima wozolowera kusirira; ana a temberero; 2 Petro 2:1,14)

Baibulo limachenjeza kuti:

Pakuti ukayamba ndi mkazi wadama, udzamariza ndi nyenyeswa; Ndipo mkazi wa mwini amasaka moyo wa mtengo wapatari. (... Miyambi 6:26)

DAMA

Dama ndi mchitidwe ogonana pakati pa anthu amene sanakwatirane. Komanso zizi zikhoza kukhala kugonana pakati pa munthu okwatira ndi osakwaitira. Zinthu zina zimene ndi mbali imodzi ya dama ndi kugona pakati pa munthu wamkazi ndi mkazi mzake kapena mamuna ndi mamuna mzake.

Dama likhoza kukhala chifukwa chokwanira chothetsera banja malingana ndi Baibulo.

koma Ine ndinena kwa inu, kuti 4 yense wakucotsa mkazi wace, kosati cifukwa ca cigololo, amcititsa cigololo: ndipo amene adzakwata wocotsedwayo acita cigololo. (Mateyu 5:32)

Anthu onse adama sadzalowa ufumu wa Mulungu:

**Kapenasimudziwa kuti osalungama sadzalandira ufumu wa Mulungu?
Musasoceretsedwe; adama, kapena opembedza mafano, kapena acigololo, kapena olobodoka ndi zoipa, kapena akudziipsa ndi amuna, kapena ambala, kapena osirira, kapena oledzera, kapena olalatira, kapena olanda, sadzalowa Ufumu wa Mulungu. (1 Akorinto 6:9-10)**

Baibulo limatiuza kuti tikuyenera kupewa dama lilironse:

Pakuti ici ndi cifuniro ca Mulungu, ciyeretso canu, kuti mudzipatule kudama; (1 Atesalonika 4:3)

Koma cifukwa ca madama munthu yense akhale naye mkazi wa iye yekha, ndi mkazi yense akhale naye mwamuna wa iye yekha. (1 Akorinto 7:2)

Kapena tisacite dama monga ena a iwo anacita dama, nagwa tsiku limodzi zikwi makumi awiri ndi zitatu. (1 Akorinto 10:8)

Thupi lamunthu silopangira dama chifukwa ndi la Mulungu. Kotero tiyenera kupewa dama:

Zakudya ndizo za mimba, ndi mimba ndiyo ya zakudya; koma Mulunguadzathera iyi ndi izi. Koma thupi siliri la cigololo, koma la Ambuye, ndi Ambuye wa thupi; Thawani dama. Cimo liri lonse munthu akalicita liri kunja kwa thupi; koma waciwerewere acimwira thupi lace la iye yekha. Pakuti munagulidwa ndi mtengo wace wapatali; cifukwa cace lemekezani Mulungum'thupi lanu. (1 Akorinto 6:13,18,20)

Ndi udindo wanthu kuthana ndi dama:

Cifukwa cace fetsani zivalozo ziri padziko; dama, cidetso, cifunitso ca manyazi, cilakolako coipa, nelicisiro, cimene ciri kupembedza mafano; (Akolose 3:5)

Dama silikuyenera ngakhale kutchulidwa kumene pakati pa okhulupirira:

Cifukwa cace fetsani zivalozo ziri padziko; dama, cidetso, cifunitso ca manyazi, cilakolako coipa, nelicisiro, cimene ciri kupembedza mafano; (Akolose 3:5)

Ngati munthu angapitilire kichitabe dama, chikumbumtima chake chimafa kotere kuti samaonanso vuto linalilironse.

Cifukwa ca ici Mulunguanawapereka iwo 1 ku zilakolako za manyazi; pakuti angakhale akazi ao anasandutsa macitidwe ao a cibadwidwe akhale macitidwe osalingana ndi cibadwidwe: anadzala ndi zosalungama zonse, kuipa, kusirira, dumbu; odzala ndi kaduka, mbanda, ndeu, cinyengo, udani; (Aroma 1:26,29)

CHIDETSO

Chidetso ndi mau otsutsana mmatanthauzo ndi mau oti: ukhondo. Malinga ndi ndime imene ikukamba za ntchito zakuthupi, mau oti “chidetso” akuimilira chidetso cha moyo wauzimu komanso makhalidwe.

Mulungu samakondwera kuti anthu ake akhale odetsedwa:

ndipo yendani m'cikondi monganso Kristu anakukondani inu, nadzipereka yekha m'malo mwathu, copereka ndi nsembe kwa Mulungu, ikhale pfungo lonunkhira bwino. (Aefeso 5:2)

Pakuti Mulungusanaitana ife titsate cidetso, koma ciyeretso. (1 Atesalonika 4:7)

Ndi udindo wathu kuchotsa chidetso china chilichonse komanso kudzipatsa mwambo ndi cholinga choti tikhale moyo wachiyero.

Cifukwa cace fetsani ziwalozi ziri padziko; dama, cidetso, cifunitso ca manyazi, cilakolako coipa, nelicisiriro, cimene ciri kupembedza mafano; (Akolose 3:5)

Pokhala nao tsono malonjezano amenewa, okondedwa, tidzikonzere tokha kuleka codetsa conse ca thupi ndi ca mzimu, ndi kutsirfza ciyero m'kuopa Mulungu. (2 Akorinto 7:1)

yense wa inu adziwe kukhala naco cotengera cace m'ciyeretso ndi ulemu, (I Thessalonians 4:4)

Ngati simungachotse kapena kuthana ndi chidetso, mapeto ake kumakhala kugwa:

Ndilankhula manenedwe a anthu, cifukwa ca kufoka kwa thupi lanu; pakuti monga inu munapereka ziwalo zanu zikhale akapolo a conyansa ndi a kusayeruzika kuti zicite kusayeruzika, inde kotero tsopano perekani ziwalo zanu zikhale akapolo a cilungamo kuti zicite ciyeretso... (Aroma 6:19)

Ngati munthu apitilira kukhalabe moyo odetsedwa kapena wuchimo, Mulungu amamusiya munthuyo kapena kumpereka kuzimtchito zake:

Cifukwa cace Mulungu anawapereka iwo m'zilakolako za mitima yao, kuzonyansa, kucititsana matupi ao wina ndi mnzace zamanyazi; (Aroma 1:24)

Pamene Mulungu wampereka munthu kuzilakolako zake, chikumbumtima chake chimafa ndipo munthuyo amalamuliridwa ndi zilakolako zake zauchimo. Munthu ameneyu amaonongeka muchimo wake pokhapokha atalapa:

Momwemo abale, onjezani kucita cangu kukhazikitsa maitanidwe ndi masankhulidwe anu; pakuti mukacita izi, simudzakhumudwa nthawi zonse; Mwa ici sindidzaleka kukukumbutsani inu nthawi zonse za izi, mungakhale muzidziwa nimukhazikika m'coonadi ciri ndi inu. (2 Petro 1:10,12)

Onani mdandanda wazinthu uli pansipa. Mukhoza kuona kuti pamene zinthu zokhudza chidetsa zabwera pamodzi, pali chinthu chimodzo chimene chikuonekera mu ndime zonsezi. Muli ndi mphamvu yothana ndi tchimo kapena kukodwa nalo tchimolo. Ngati mungathane ndi chidetso, izi zimakuthandizani kuti mukhale moyo wachiyero. Pamene Mulungu watipereka kuchidetso chathu, mapeto ake amakhala chiongeko chifukwa chachinyengo chathu.

Ngati

Mungachotse chidetso:



Akolose 3:5

Zotsotira zake ndi

Chiyero

I Atesalonika 4:7

chanu:

Ngati

Mungagonjere ku zinthu zonyansa

Aroma 6:19

Zotsatira zake ndi

Kudzipereka nokha kuchonyasa

Aefeso 4:19.

Zotsatira zake ndi.

Mulunguamakuperekani ku zonyansa zanu

Zotsatira zake ndi chionongeko muchivundi

II Petro 2:10,2.

CHILAKOLAKO CHONYANSA

Chilakolako chonyansa ndi tchimo lokhala ndi chikhumbitso chonyasa chochita zinthu mopanda manyazi. Chilakolako chonyansa ndi chikhalidwe chimodzi chimene chimaonekera mwa aphunzitsi onyenga.

Pakuti pali anthu ena anakwawira m'tseri, ndiwo amene aja adalembedwa maina ao kale, kukalandira citsutso ici, anthu osapembedza, akusandutsa cisomo ca Mulunguwathu cikhale cilak olako conyansa, nakaniza Mfumu wayekha, ndi Ambuye wathu, Yesu Kristu. (Yuda 1:4)

Mu nthawi yakale mwina mkutheka munayenda muzilakolako zonyasa. Koma ngati Okhulupirira simukuyenera kuyendanso mumakhalidwe amenewa.

kuti nthawi yotsalira simukakhalenso ndi moyo m'thupi kutsata zilakolako za anthu, koma cifuniro ca Mulungu. Pakuti nthawi yapitayi idatifikira kucita cifuno ca amitundu, poyendayenda ife m'kukhumba zonyansa, zilakolako, maledzero, madyerero, mamwaimwa, ndi kupembedza mafano kosaloleka;(1 Petro 4:2-3)

Baibulo limaphunzitsa kuti ngati munthu angapitilire kuyendabe mu zilakolako zonyasa, mapeto ake mumadzipereka nokha kuchikhalidwe chimenechi ndipo chikumbumtima chanu chimafa.

amenewo popeza sazindikiranso kanthu konse, anadzipereka okha kuti akhumbwe zonyansa, kuti acite cidetso conse mu umbombo. (Aefeso 4:19)

MAFANO

Mafano ndi mtchitidwe opembedza milungu. Izi simatanthauza kupembedza fano losemedwa kaya kucholera kumtengo kapena mwala. Fano ndi chinthu chinachirichonse chimene

chimakhala chofunika kuposa Mulungu. Anthu amafano ndi anthu amene amapembedza zinthu zina kupatula Mulungu weniweni. Kupembedza mafano ndi kulephera kuzindikira mala ake a Mulungu mmoyo wanu.

Limodzi mwa malamuro oyamba amene Mulungu anapereka limakhudza mafano:

Musamatembenukira mafano, kapena kudzipangira Mulunguwoyenga; Ine ndine Yehova Mulunguwanu. (Levitiko 19:4)

Musamadzipangira mafano, kapena kudziutsira mafano osema, kapena coimiritsa, kapena kuika mwala wozokota m'dziko mwanu kuugwadira umene; popeza Ine ndine Yehova Mulunguwanu. (Levitiko 26:1)

Milungu yonse ya amitundu imatchedwa mafano:

Pakuti milungu yonse ya mitundu ya anthu ndiyo mafano: Koma Yehova analenga zakumwamba. (Masalmo 96:5)

Mumasokonekera ngati mungatumikire mafano:

Onse akutumikira fano losema, Akudzitamandira nao mafano, acite manyazi: Mgwadireni Iye, milungu yonse inu. (Masalmo 97:7)

Mafano a anthu amitundu ndi ntchito zamanja awo. Amakhala opanda mphamvu kapena kufunika kwina kulikonse:

Mafano a amitundu ndiwo siliva ndi golidi, Nchito ya manja a anthu. Pakamwa ali napo koma osalankhula; Maso ali nao, koma osapenya; Makutu ali nao, koma osamva; Inde, pakamwa pao palibe mpweya. Akuwapanga adzafanana nao; Inde, onse akuwakhulupirira. (Masalmo 135:15-18).

Khristu sayenera kupembedza mafano:

**Ndipo ciphatikizo cace ncanji ndi kacisi wa Mulungundi wa mafano?
(2 Akorinto 6:16)**

Simukuyenera kuchita ubwenzi ndi anthu opembedza mafano:

**koma tsopano ndalemba inu kuti musayanjane naye, ngati wina wochedwa mbale ali wacigololo, kapena wosirira, kapena wopembedza mafano, kapena wolalatira, kapena woledzera, kapena wolanda, kungakhale kukadya naye wotere, iai.
(1 Akorinto 5:11)**

Anthu onse opembedza mafano sadzalowa Ufumu Wakumwamba.

**Kapenasimudziwa kuti osalungama sadzalandira ufumu wa Mulungu?
Musasoceretsedwe; adama, kapena opembedza mafano, kapena acigololo, kapena olobodoka ndi zoipa, kapena akudziipsa ndi amuna, kapena ambala, kapena osirira, kapena oledzera, kapena olalatira, kapena olanda, sadzalowa Ufumu wa Mulungu.
(1 Akorinto 6:9-10)**

Baibulo limaonetsera chimaliziro cha anthu opembedza mafano:

Koma amantha, ndi osakhulupira, ndi onyansa, ndi ambanda, ndi acigololo, ndi olambira mafano, ndi onse a mabodza, colandira cao cidzakhala m'nyanja yotentha ndi mota ndi sulfure; ndiyo imfa yaciwiri. (Cibvumbulutso 21:8)

Kunja kuli agaru ndi anyanga, ndi acigololo, ndi ambanda, ndi opembedza mafano, ndi yense wakukonda bodza ndi kulicita. (Cibvumbulutso 22:15)

Baibulo limafotokoza kuti kuti kusilira ndi chimodzimodzi kupembedza mafano. Kusilira ndi kusilira chinthu ndi cholinga cholakwika. Muyenera kulimbana kapena kuthana ndi kusilira:

Cifukwa cace fetsani zivalozo ziri padziko; dama, cidetso, cifunitso ca manyazi, cilakolako coipa, nelicisiriro, cimene ciri kupembedza mafano; (Akolose 3:5)

Ndikutheka kuti munali munthu opembedza mafano, koma okhulupirira sayenera kupitira kuyendabe mumafano:

kuti nthawi yotsalira simukakhalenso ndi moyo m'thupi kutsata zilakolako za anthu, koma cifuniro ca Mulungu. Pakuti nthawi yapitayi idatifikira kucita cifuno ca amitundu, poyendayenda ife m'kukhumba zonyansa, zilakolako, maledzero, madyerero, mamwaimwa, ndi kupembedza mafano kosaloleka; (1 Petro 4:2-3)

Pakuti iwo okha alalikira za ife, malowedwe athu a kwa inu anali otani; ndi kuti munatembeoukira kwa Mulunguposiyana nao mafano, kutumikira Mulunguweni weni wamoyo, (1 Atesalonika 1:9)

UFITI

Ufiti ndi mtchitidwe umene afiti machita. Zinthu zina zimene ndi mbali imodzi ya Yaufiti ndi matsenga, nyanga, kulodza ndi kugwiritsa ntchito mwakhala. Kupembedza Satana komanso mtchitidwe wina ulionse okhudzana ndi Satana ndi mbali imodzi ya Ufiti.

Tikhoza kuonjezera kuti ufiti ndi kuwapanga anthu kuti apange zinthu zimene sakufuna koma asakudziwa. Ngakhale kuti simumachita mchitidwe waufiti, mukhoza kumachimwa ntchimo laufiti ngati mungamapemphere pemphero lotsutsana ndi anthu ena.

Ufiti ndi kuukila Mulungu kwauzimu. Mulungu amati ntchimo la kuukila ndi chimodzimodzi ufiti.

kuti nthawi yotsalira simukakhalenso ndi moyo m'thupi kutsata zilakolako za anthu, koma cifuniro ca Mulungu. Pakuti nthawi yapitayi idatifikira kucita cifuno ca amitundu, poyendayenda ife m'kukhumba zonyansa, zilakolako, maledzero, madyerero, mamwaimwa, ndi kupembedza mafano kosaloleka; (1 Petro 4:2-3)

Pakuti iwo okha alalikira za ife, malowedwe athu a kwa inu anali otani; ndi kuti munatembeoukira kwa Mulunguposiyana nao mafano, kutumikira Mulunguweni weni wamoyo, (1 Atesalonika 1:9)

MADANO

Mau oti madano ndi otsutsana mmatantauzo ndi mau oti chikondi. Madano ndi kukhala ndi chidani chachikulu kapena kuipidwa ndi anthu ena. Baibulo limafotokoza kuti madano amabweretsa kupikisana kapena kui mpikisano pakati pa anthu:

Udani upikisanitsa; Koma cikondi cikwirira zolakwa zonse. (Miyambi 10:12)

Ndi kwabwino kukhala malo emene pali chikondi kusiyana ndi kukhala pakati pa anthu odzadzidwa ndi ndi madano.

Kudya masamba, pali cikondano, Kuposa ng'ombe yonenepa pali udani. (Miyambi 15:17)

Madano obisika ndi chinyengo adzabweleretsedwa poyera ndi Mulungu:

Angakhale abisa udani wace pocenjera, Koma udio wace udzabvumbulutsidwa posonkhana anthu. (Miyambi 26:26)

Pamene munali osakhulupirira, munali ana amkwiyo:

amene ife tonsenso tinagonera pakati pao kale, m'zilakolako za thupi lathu, ndi kucita zifuniro za thupi, ndi za maganizo, ndipo tinali ana a mkwiyo cibadwire, monganso otsalawo; (Aefeso 2:3)

Koma simukuyeneranso kukhala ana a mkwiyo:

Ciwawo conse, ndi kupsya mtima, ndi mkwiyo, ndi ciwawa, ndi mwano zicotsedwe kwa inu, ndiponso coipa conse. (Aefeso 4:31 11)

Koma muyenera kuchotsa mkwiyo:

Koma olakwa adzaonongeka pamodzi: Matsiriziro a oipa adzadutidwa. (Masalmo 37:38)

Muyenera kucedwa kukwiya:

Mudziwa, abale anga okonedwa, kuti munthu ali yense akhale wochera khutu, wodekha polankhula, wodekha pakupsa mtima. Pakuti mkwiyo wa munthu sucita cilungamo ca Mulungu. (Yakobo 1:19-20)

Wosakwiya msanga apambana kumvetsa; Koma wansontho akuza utsiru. (Miyambi 14:29)

Pali kugwirizana kwakuku pakati pa mkwiyo ndi mfundo yachiwiri yokhudza ntchito zakuthupi. Baibulo limafotokoza kugwirizana pakati pa makangano/ makani ndi madano.

Munthu wozaza aputa makani; Koma wosakwiya msanga atonthoza makangano. (Miyambi 15:18)

Pakuti potakasa mkaka, mafuta ayengekapo; Ndi popsinja mpfuno, mwazi uturukamo; Ndi potimbikira mkwiyo ndeu ionekamo. (Miyambi 30:33)

MAKANI/ MAKANGANO

Makani ndi kukangani, kumenyana kapena kusagwirizana. Makani akhoza kukhala milandu kapena kusamvana pakati pa anthu. Kuonjezera mkwiyo umene umayambitsa makakangano, madano amathanso kuyambitsa makangano.

Udani upikisanitsa; Koma cikondi cikwirira zolakwa zonse. (Miyambi 10:12)

Munthu okhota amautsa makani kapena kuti makangano:

Munthu wokhota amautsa makani; Kazitape afetsa ubwenzi. (Miyambi 16:28)

Kudzikuza kumayambitsa makangano:

Wodukidwa mtima aputa makangano; Koma wokhulupirira Yehova adzakula. (Miyambi 28:25)

Munthu okwiya amatha kuyambitsa makangano:

Mwini diso lankhwenzule akangaza kulemera, Osadziwa kuti umphawi udzamfikira. (Miyambi 28:22)

Munthu onyoza amayambitsa makangano:

Ukainga wonyoza, makangano adzaturuka; Makani ndi manyazi adzalekeka. (Miyambi 22:10)

Kukhala munthu onyoza ndi kusalemekeza chinthu kapena munthu winawake.

Anthu amene amalowelera zinthu zosawakhudza komanso okonda kutsutsana kapena kukamba za anthu ena amayambitsa makangano:

Wakungopita ndi kubvutika ndi ndeu yosakhala yace Akunga wogwira makutu a garu. Posowa nkhuni moto ungozima; Ndi popanda kazitape makangano angoleka. Monga makala ozizira pa makala akunyeka, ndi nkhuni pamoto; Momwemo munthu wamakangano autsa ndeu. (Miyambi 26:17,20-21)

Mafuso opusa amatha kubweleretsa makangano:

Koma mafunso opusa ndi opanda malango upewe, podziwa kuti abala ndeu. (II Timoteo 2:23)

Makangano ndi ntchito yakuthupi:

pakuti, pokhala pali nkhwidzi ndi ndeu pakati pa inu simuli athupi kodi, ndi kuyendayenda monga mwa munthu? (1 Akorinto 3:3)

Pamene pali kaduka ndi madano, pamakhalanso chisokonekero:

musacite kanthu monga mwa cotetana, kapena monga mwa ulemerero wopanda pace, komatu ndi kudzicepetsa mtima, yense ayese anzace omposa iye mwini; (Afilipi 2:3)

Makangano ndi chikhalidwe chimodzi chimene aphunzitsi onyenga amaonetsera.

iyeyo watukumuka, wosadziwa kanthu, koma ayarukira pa mafunso ndi makani a mau, kumene zieokerako njiru, ndeu, zamwano, mayerekezo oipa; makani opanda pace a anthu oipsika nzeru ndi ocotseka coonadi, akuyesa kuti cipembedzo cipindulitsa. (1 Timoteo 6:4-5)

CHIPHUNZITSO CHONYENGA

Chiphunzitso chonyenga ndi chikhulupiriro chinachilichonse chimene chili chosemphani ndi Mau a Mulungu. Awa amakhala maganizo a munthu amene amakhala olakwika. Chiphunzitso chonyenga ndi chizindikiro chimodzo cha aneneri onyenga:

Koma padakhalanso pakati pa anthuwo aneneri onama, monganso padzakhala aphunzitsi onama pakati pa inu, amene adzalowa nayo m'tseri mipatuko yotayikitsa, nadzakana Ambuye amene adawagula, nadzadzitengera iwo okha citayiko cakudza msanga.... (2 Petro 2:1)

KADUKA

Kaduka ndi nsanje imene imabwera chifukwa chakuchita bwino kwa anthu ena. Ndi kutsutsana ndi mdalitso wa anthu ena mmagawo ena monga kuthupi, zachuman ndi zina zambiri.

Kaduka ndi chikhalidwe chimodzi cha aphunzitsi onyenga:

iyeyo watukumuka, wosadziwa kanthu, koma ayarukira pa mafunso ndi makani a mau, kumene zieokerako njiru, ndeu, zamwano, mayerekezo oipa; (1 Timoteo 6:4)

Kaduka gwero lake ndi mzimu wa munthu:

Akazi acigololo inu, kodi simudziwa kuti ubwenzi wa dziko lapansi uti udani ndi Mulungu? Poto, iye amene afuna kukhala bwenzi la dziko lapansi adziika mdani wa Mulungu. (Yakobo 4:4)

Kaduka ndi chizindikiro chokhala okhulupira wakuthupi:

pakuti, pokhala pali nkhwidzi ndi ndeu pakati pa inu simuli athupi kodi, ndi kuyendayenda monga mwa munthu?? (Corinthians 3:3)

Anthu amakhala moyo wauchimu amakhala odzadzidwa ndi Kaduka:

anadzala ndi zosalungama zonse, kuipa, kusirira, dumba; odzala ndi kaduka, mbanda, ndeu, cinyengo, udani; ... (Aroma 1:29)

Pakuti kale ifenso tinali opusa, osamvera, onyengeka, akucitira ukapolo zilakolako ndi zokondweretsa za mitundu mitundu, okhala m'dumbo ndi njiru, odanidwa, odana wina ndi mnzace. (Tito 3:3)

Pamene pali kaduka pamakhala mavuto ambiri:

Koma mukakhala nako kaduka kowawa, ndi cotetana m'mtima mwanu, musadzitamandira, ndipo musamanama potsutsana naco coonadi. Pakuti pomwe pali kaduka ndi zotetana, pamenepo pali cisokonekero ndi cocita coipa ciri conse. Yakobo 3:14,16

Timachenjezedwa kuti sitikuyenera kusilira kapena kuchita kaduka ndi anthu ochimwa:

Mtima wako usacitire nsanje akucimwawo; Koma opabe Yehova tsiku lonse; (Miyambi 23:17)

ANTHU AKUPHA

Kupha ndi kutenga moyo wa munthu wina ndi cholinga choipa. Kupha ndi kosiyana ndi kudziteteza nokha kapena kupha mwangozi. Kupha munthu wina ngati chilango chifukwa choti wapha munthu wina sikupha. Ichi ndi chilango chimene Mulungu anakhazikitsa pa Numeri 35. Limodzi mwa malamuro oyamba amene Mulungu anapereka linali loti usaphe.

Yesu anati:’

Iye ananena kwa Iye, Otani? Ndipo Yesu anati, Usaphe, (Mateyu 19:18)

Simukuyenera kukhala olakwa pa mlandu wakupha.

Pakuti asamve zowawa wina wa inu ngati wambanda, kapena mbala, kapena wocita zoipa, kapena ngati wodudukira; (1 Petro 4:15)

Chipangano Chatsopano chimafotokoza tanthauzo la Kupha kuti kukhala ndi chidani ndi okhulupirira ena ndi chimodzimodzi kupha.

Yense wakudana ndi mbale wace ali wakupha munthu; ndipo mudziwa kun wakupha munthu ali yense alibe moyo wosatha wakukhala mwa iye. (1 Yohane 3:15)

KULEDZERA

Kuledzera ndi pamene maganizidwe athu komanso thupi lathu limasokonekera chifukwa chomwa mowa kwambiri. Baibulo limachenjeza kuti anthu oledzera adzasauka:

Pakuti wakumwaimwa ndi wosusukayo adzasauka; Ndipo kusinza kudzabveka munthu nsanza.... (Miyambi 23:21)

Simukuyenera kukhala moyo wauchidakwa:

Tiyendeyeode koyenera, monga usana; si m'madyerero ndi kuledzera ai, si m'cigololo ndi conyansa ai, si mu ndeu ndi nkhwidzi ai. (Aroma 13:13)

Simukuyenera kuchita ubwenzi ndi anthu oledzera:

koma tsopano ndalemba inu kuti musayanjane naye, ngati wina wochedwa mbale ali wacigololo, kapena wosirira, kapena wopembedza mafano, kapena wolalatira, kapena woledzera, kapena wolanda, kungakhale kukadya naye wotere, iai. (1 Akorinto 5:11)

Baibulo limachenjeza kuti oledzera onse sakalowa Ufumu wa Mulungu:

Kapenasimudziwa kuti osalungama sadzalandira ufumu wa Mulungu? Musasoceretsedwe; adama, kapena opembedza mafano, kapena acigololo, kapena olobodoka ndi zoipa, kapena akudziipsa ndi amuna, kapena ambala, kapena osirira, kapena oledzera, kapena olalatira, kapena olanda, sadzalowa Ufumu wa Mulungu. (1 Akorinto 6:9-10)

Mwina mkutheka kuti muli oledzera mbuyomu, koma ngati okhulupirira simukuyeneranso kukhala mmoyo umeu:

kuti nthawi yotsalira simukakhale ndi moyo m'thupi kutsata zilakolako za anthu, koma cifuniro ca Mulungu. Pakuti nthawi yapitayi idatifikira kucita cifuno ca amitundu, poyendayenda ife m'kukhumba zonyansa, zilakolako, maledzero, madyerero, mamwaimwa, ndi kupembedza mafano kosaloleka; (1 Petro 4:2-3)

Baibulo limasiyanitsa kuledzera ndi vinyo ndi kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera.

Ndipo musaledzere naye vinyo, m'mene muli citayiko; komatu mudzale naye Mzimu, (Aefeso 5:18)

Munthu oledzera Kudziko lakuthipi...

1. Amatengedwa ndi chilakolako choti amwe.
2. Maganizidwe kapena thupi lake zimakhala pansu pa ulamuliro wa chakumwa.
3. Malankhalidwe ake amasokonekera ndi chakumwa.
4. Amakhala kuti alibe kudziletsa kwina kulikonse. Amakhala ndi mphamvu zambiri.
5. Amakhala ndi chisangalalo akakhala kuti waledzera.

KUKHUMBA ZONYANSA

Kukhumba zonyasa ndi kuchita ndi kukondwera ndi zinthu zosangalatsa thupi koma zachikunja kapena kuti za dziko lapansi. Tikhoza kufotokozanso kuti chikhumbitso chonyasa ndi kukhala ndi moyo wachisawawa okowendwelera muzinthu zonyasa.

Mkutheka kuti mumakhala muzinthu zonyansa kalero, koma ngati okhulupirira simukuyeneranso kukhala mizinthu zimenezi.

kuti nthawi yotsalira simukakhalenso ndi moyo m'thupi kutsata zilakolako za anthu, koma cifuniro ca Mulungu. Pakuti nthawi yapitayi idatifikira kucita cifuno ca amitundu, poyendayenda ife m'kukhumba zonyansa, zilakolako, maledzero, madyerero, mamwaimwa, ndi kupembedza mafano kosaloleka;(1 Petro 4:2-3)

NTCHITO ZAKUTHUPI: ZOTSATIRA ZAKE

Paulo akufotokoza zotsatira za ntchito yakuthupi:

zimene ndikucenjezani nazo, monga ndacita, kuti iwo akucitacita zotere sadzalowa Ufumu wa Mulungu. (... Agalatiya 5:21)

Mulungu anapereka njira yoti tipewere chilango choyenda kuthupi.

Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse. (1 Yohane 1:9)

KUYENDA MUMZIMU

Kodi muthu angasiye bwanji kuchita ntchito zakuthupi:

Choyamba: Munthu ayenera kulapa machimo ake ndikuvomereza Yesu ngati mpulutsi.

Cifukwa cace ngati munthu ali yense ali mwa Kristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano, (2 Akorinto 5:17)

Sikuti pamakahala maphunziro apadera amene Mulungu amapereka kwa munthu ochimwa kuti adzikonze yekha. Iye amapereka chikhalidwe chatsopano, zinthu zakale zimakhala kuti zapita. Ntchito zakuthupi zikuyenera kusithanitsidwa ndi chipatso cha Mzimu Woyera.

Chachiwiri: Kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Ndi Mzimu Woyera amene amatithandiza kuti tiyende munjira ya Mzimu osati mu njira zakuthupi.

Pakuti thupi lilakalaka potsutsana naye Mzimu, ndi Mzimu potsutsana nalo thupi; pakuti izi sizilingana; kuti zimene muzifuna musazicite. (Agalatiya 5:17)

Chachitatu: Muyenera kuzindikira kuti simungathe kudzimasula nokha ku ntchito zakuthupi ndi kuyamba kuyenda mwa Mzimu Woyera.

Mtumwi Paulo akufotokoza kulimbana kumene kunali mkati mwake pofuna kuyenda moyo wauzimu pogwiritsa ntchito kuthekera kakwe:

Pakuti cimene ndicita sindicidziwa; pakuti sindicita cimene ndifuna, koma cimene ndidana naco, ndicita ici. Koma ngati ndicita cimene sindicifuna, ndibvomerezana naco cilamulo kuti ciri cabwino. Ndipo tsopano si ine ndicicita, koma ucimo wakukhalabe m'kati mwanga ndiwo. Pakuti ndidziwa kuti m'kati mwanga, ndiko m'thupi langa, simukhala cinthu cabwino; pakuti kufuna ndiri nako, koma kucita cabwino sindikupeza. Pakuti cabwino cimene ndicifuna, sindicicita; koma coipa cimene sindicifuna, cimeneco ndicicita. (Aroma 7:15-19)

Paulo anakumana ndi kulimbana mkati mwake pofuna kukhala moyo wachiyero. Koma ngakhale kuti panali kulephera, Iye anapitirilabe moyo wake wachikhristu.

Muyenera kupempha Mulungu kuti ayikize mwainu chikhumbokhumbo chofuna kukhala moyo wachiyero. Pamene mwalephera ndikuchimwa, muyenera kulapa komanso kupempha Mzimu Woyera kuti akuthandizeni kuti mugonjetse zinthu zokulepheretsanizo. Umu ndi mmene mungaphunzilire kuyenda Munzimu.

Cifukwa cace tsopano iwo akukhala mwa Kristu Yesu alibe kutsutsidwa. Pakuti cilamulo ca mzimu wa moyo mwa Kristu Yesu candimasula ine ku lamulo la ucimo ndi la imfa. Pakuti cimene cilamulo sicinathe kucita, popeza cinafoka mwa thupi, Mulunguanatumiza Mwana wace wa iye yekha m'cifanizo ca thupi la ucimo, ndi cifukwa ca ucimo, natsutsa ucimo m'thupi; kuti coikika cace ca cilamulo cikakwaniridwe mwa ife, amene sitiwendayenda monga mwa thupi, koma monga mwa mzimu. Pakuti iwo amene ali monga mwa thupi asalalira zinthu za thupi; koma iwo amene ali monga mwa mzimu, asalalira zinthu za mzimu: pakuti cisamaliro ca thupi ciri imfa; koma cisamaliro ca mzimu ciri moyo ndi mtendere. Cifukwa cisamaliro ca thupi cidana ndi Mulungu; pakuti sicigonja ku cilamulo ca Mulungu, pakuti sicikhoza kutero. Ndipo iwo amene ali m'thupi sangathe kukondweretsa Mulungu. (Aroma 8:1-8)

Chipatso chokhala ndi chikhalidwe cha Yesu chimakula pamene mukuyenda mu mphamvu ya Mzimu Woyera. Ichi ndi chifukwa chake ndi zofunika kuti okhulupirira ayenera kumvetsetsa utumiki wa Mzimu Woyera.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

2. Chikhalidwe chosiyana cha chipatso cha Mzimu Woyera chimatchedwa:

3. Kodi ndi vesi yanji m’Baibulo imene ndiyofunika pothana ndi ntchito zathupi.

4. Patsamaba liri pansipa, werengani ntchito zakuthupi mu mdandanda oyamba. Ndipo werengani matanthauzo amene akupezeka mu mdandanda wachiwiri. Lembani namabala imene ikufotokoza ntchito yakuthupi pa mpata umene waperekedwa.

Mdandanda oyamba

___ Zoopsa mtima

___ Kaduka:

___ Akupha

___ Kuledzera

___ Kukhumba zonyasa

___ Chigoloro

___ Dama

___ Chidetso

___ Ufiti

___ Mafano

___ Madano

___ Mipatuko

___ Chiphunzitso chonyenga

___ Kaduka/kutengera

___ Ndeu/

___ Mkwiyu

___ Kunyoza

mdandanda wachiwiri

1. Kugonana pakati pa munthu okwatira ndi munthu amene simkazi wao

2. Kugonana pakati pa anthu awiri amene sanakwatirane.

3. Machimo akuthupi ndi kuuzimu komwe.

4. Chilakolako, maganizo auchimo, chonyansa.

5. Kupembedza mafano.

6. Mtchitidwe wa afiti. _____

7. Mau otsutsana matanthauzo ndi chikondi.

8. Kusagwirizana kapena kusamvana

9. Mchitidwe ofuna kupikisana ndi ena potendera zimene akuchita ndicholinga chofuna kufanana nao kapena kuwapambana iwo

10. Mkwiyu waukulu komanso kupsa mtima.

11. Kukangana kapena kumenya

12. Kubweretsa mpungwepungwe kusagwirizana.

13. Zikhulupiriro zosemphana ndi Mau a Mulungu.

14. Nsanje chifukwa chakuchita bwino kwa anthu ena.

15. Kuchotsa moyo wa munthu wina

16. Kumwa mwauchidakwa.

17. Chikunja, chisawawa chokondweretsa thupi.

(mayankha amafunso awa ali kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Siyanitsani chipatso chauzimu pa Agalatiya 5:22-24 ndi ntchito zakuthupi zimene zatchulidwa pa Agalatiya 5:12-21. Yango loyamba laperekedwa ngati chitsanzo choti chitsatidwe

KUSIYANA

**Chipatso chauzimu
(Agalatiya 5:22-24)**

**Ntchito zakuthupi
(Agalatiya 5:19-21)**

Chikondi

Madano, kuphana, kaduka

Chimwemwe

Mtendere

Chipiriro

Kukoma mtima

Chifundo

Chikhulupiriro

Chifatso

Chiletso

CHAPUTALA 13

KUKUZA CHIPATSO CHANU CHAUZIMU

ZOLINGA:

Pamapeto paphunziro ili muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kufotokoza mlingo osiyasiyana wakabalidwe kachipatso chauzimu.
- Kugwiritsa ntchito zitsanzo zakuthupi zakabalidwe kazipatso pofuna kufotokozero mmene chipatso chauzimu chimakulira mmoyo wa munthu okhulupirira.

VESI YOTSOGOLERA

Nthambi iri yonse ya mwa Ine yosabala cipatso, aicotsa; ndi iri y'onse yakubala cipatso, aisadza, kuti ikabale cipatso cocuruka. (Yohane 15:2)

CHIYAMBI

Vesi yotsogolera ya chaputala ichi ikuchutira umboni kuti cholinga cha Mulungu ndichakuti chipatso chauzimu chiyenera kuonekera mmoyo wanu. Chaputala ichi chikupereka ndondondomeko zothandiza kuti mukuze chipatso chauzimu.

MLINGO WAKABALIDWE KACHIPATSO CHAUZIMU

Pali mlingo osiyanasiya wakabalidwe kazipatso zauzimu zimene ziyenera kuonekera mmoyo wa munthu okhulupirira. Yohane 15 akufotokoza mlingo osiyanasiya wakabalidwe kachipatso chauzimu.

- Chipatso Yohane 15:2a
- Zipatso zambiriko: Yohane 15:2b
- Zipatso zochulukitsitsa: Yohane 15:5, 8
- Chipatso chokhazikika: Yohane 15:16

Cholinga cha Mulungu ndi chakuti mubale zipatso zambiri zimene ndi zokhazikika. Iye akufuna kuti mupindule kwambiri muchipatso chanu chooneka chakulalikira uthenga Wabwino ndi chipatso chamkati chokhala ndi makhalidwe angati a Yesu Khristu.

CHOONADI CHAKUTHUPI NDI CHAUZIMU

Baibulo liri ndi mfundo zofunika kwambiri zimene muyenera kuzizindikira kuti mukathe kumvetsa chimene Mulungu akufotokoza kudzera mmau ake. Imodzi mwa mfundo imeneyi ndi kufanana kwa choonadi chakuthupi ndi chauzimu. Mulungu amagwiritsa ntchito choonadi chakuthupi pofuna kuonetsera choondai chauzimu.

Mafanizo a Yesu Khristu ndi ndi chitsanzo chimodzi cha choonadi chakuthupi chofotokera choonadi chauzimu. Mwachitsano, mufanizo lina Yesu Khristu anagwiritsa ntchito fanizo la mzimayi ofunafuna ndalama yotaika. Yesu anagwiritsa ntchito chitsanzo chimenechi pofuna

kuonetsera chidwi chimene tikuyera kukhala nacho pofunafuna anthu otaika. Ili ndi fanizo limodzi mwa mafanizo ambiri amene Yesu anagwiritsa ntchito pofuna kuonetsera choonadi chاوزimu.

Mfundo yakufanana kwa choonadi chakuthupi ndi choonadi chاوزimu zikufotokeredwa pa 1 Akorinto:

Ngati pali thupi Iacibadwidwe, palinso lauzimu. Koteronso kwalembedwa, 11 Munthu woyamba, Adamu, anakhala mzimu wamoyo. 12 Adamu wotsirizayo anakhala mzimu wakulenga moyo. Koma cauzimu siciri coyamba, koma cacibadwidwe; pamenepo cauzimu. (1 Akorinto 15:44-46)

Mu ndime imeneyi Mtumwi Paulo anapereka chimodzi mwa zitsanzo chopambana chachitsazo chakuthupi choonetsera choonadi chاوزimu. Munthu oyamba amene ndi Adamu anali munthu wakuthupi. Koma Yesu amene ndi Adamu wachiwiri kapena omaliza anali wاوزimu. Adamu anali chitsanzo chakuthupi choonetsera choonadi chاوزimu cha Mulungu kudzera mwa Yesu Khristu. Kudzera mwa munthu wakuthupi tchimo ndi imfa zinalowa pa dziko lapansi. Chimodzimodzinso kudzera mwa munthu wاوزimu chipulumutso chinadza kwa anthu onse.

Chinthu chakuthupi ndi chimene chimaoneka ndi maso, chimene mungathe kuchigwira kapena kuchimva. Koma chinthu chاوزimu ndi chimene chisimaoneka ndi maso. Chitsanzo chakuthupi ndi chimene munthu akhoza kuchizindikira ndi zinthu zakuthupi monga maso kapena makutu. Pamene chitsanzo chakuthupi chimazindikiridwa ndi vumbulutso la Mzimu Woyera. Kumvetsetsa mfundo ya kufanana pakati pa choonadi chakuthupi ndi chاوزimu ndi kofunika chifukwa zimathandiza kulandira kumvetsetsa kwina kwa mau a Mulungu.

KUKUZA CHPATSO CHAUZIMU:

Yesu anangwiritsa ntchito mau oti “Chipatso chاوزimu ngati chitsanzo chakuthupi pofuna kuonetsera choonadi chاوزimu. Pali zinthu zina zimene zimayenera kukhalapao kuthupi kuti kuti pakhale kukula. Ndipo izi ndi chimodzimodzinso kudziko lauzimu. Zinthu zimene zimayenera kukhalapo kuti pakhale kukula ndi izi:

MOYO

Chinthu choyamba kuti pakhale kukula kwa chipatso chاوزimu ndi moyo. Moyo wa mbeu yakuthupi umakhala mu mbweu. Pamene moyo mu dziko lauzimu umachokera mu mbeu ya Yesu Khristu.

Mu lonjezano loyamba la mpulumutsi wa dziko lapansi, Yesu akuvumbulutsidwa ngati mbeu:

ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo, ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yace; ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira citende cace. (Genesis 3:15)

Pakuti monga Atate ali ndi moyo mwa iye yekha, momwemonso anapatsa kwa Mwana kukhala ndi moyo mwa iye yekha; (Yohane 5:26)

Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga, Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wocuruka. (Yohane 10:10)

Mbeu yamoyo imene ndi Yesu Khristu iyenera kukhala yamoyo. Ndizosatheka kubala chipatso cha Mzimu ngati mulibe ubale wina ulionse ndi Yesu Khristu.

MADZI

Ku dziko lakuthupi, madzi ndi chinthu chofunika kuti mtengo ubale chipatso. Madzi ndi chizindikiro chimodzi chimene chimaimira Mzimu Woyera. Chimodzimodzinso, madzi a Mzimu Woyera ndi ofunika kuti munthu abale chipatso chazimu. Komanso amachotsa ludzu lauzimu ndi kuthandizira kuti mukule moyo wauzimu

Iye wokhulupirira Ine, monga cilembo cinati, Mitsinje ya madzi amoyo idzayenda, kuturuka m'kati mwace. Koma 1 ici anati za Mzimu, amene iwo akukhulupirira iye anati adzalandire; pakuti Mzimu panalibe pamene, cifukwa Yesu sanalemekezedwa panthawi pomwepo. (Yohane 7:38-39)

Pakuti ndidzathira madzi pa dziko limene liribe madzi, ndi mitsinje pa nthaka youma; ndidzathira mzimu wanga pa mbeu yako, ndi mdalitso wanga pa obadwa ako; (Yesaya 44:3)

KUWALA

Kuwala kumathandiza kuti zithu zikule kapena kuti zibale. Zimatengera mmene inuyo mungachitire ndi kuunika kwa Mau a Mulungu kumene kungakupangitseni kuti mubale zipatso.

Ndipo uwu ndi uthenga tidaumva kwa iye, ndipo tiulalikira kwa inu, kuti Mulungundiye kuunika, ndipo mwa iye monse mulibe mdima. Tikati kuti tiyanjana ndi Iye, ndipo tiyenda mumdima, tinama, ndipo siticita coonadi; koma ngati tiyenda m'kuunika, mongalye ali m'kuunika, tiyanjana wina ndi mnzace, ndipo mwazi wa Yesu Mwana wace utisambitsa kuticotsera ucimo wonse. (1 Yohane 1:5-7)

MPHWEYA

Zomera zimapeza mphweya kuchokera munthaka kapena kuti kuchokera mulengalenga. Kuti mbeu ikule komanso ibale, imafuna mpweya. Malingana ndi Mau a Mulungu, Mzimu Woyera amafanananitsidwa ndi mpweya kapena mphepo:

iye wocita cimo ali wocokera mwa mdierekezi, cifukwa mdierekezi amacimwa kuyambira paciyanbi. Kukacita ici Mwana wa Mulungu adaonekera, ndiko kuti akaononge nchito za mdierekezi, (1 Yohane 3:8)

“Mphepo ya Mzimu imene ikaomba pa moyo wanu ili ngati mphepo yakuthupi. Imathandiza kufesa mbeu ya Mau a Mulungu, komanso imasiyanitsa tirigu ndi madeya a tiriguyo, imathandizira kukolezera moto wamoyo wauzimu kuti mukhale pamoto wamoyo.

MALO

Malingana fanizo la ofesa mbeu limene likupezeka pa Mateyu 13, mpikisano pakati pa mbeu unapangitsa kuti mbeu zina zitsamwe. Okhulupirira amene akufuna kukuza chipatso chauzimu ayenera kuzindikira kuti ndi kofunika kudzipatula ku mpikisanu wa padziko lapansi:

Ndipo iye amene afesedwa kuminga, uyu ndiye wakumva mau; ndipo kulabadira kwa dziko lapansi, ndi cinyengo ca cuma citsamwitsa mau, ndipo akhala wopanda cipatso. (Mateyu 13:22)

Simukuyenera kufanizidwa ndi njira za dziko lapansi. Koma mukuyenera kukhala osandulika kapena kuti osinthika malingana ndi njira za Mulungu.

Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire cimene ciri cifuno ca Mulungu, cabwino, ndi cokondweretsa, ndi cangwiro. (Aroma 12:2)

Mulungu anakonza malo amene akuzungulirani ndi cholinga choti muthe kukula moyo wanu wauzimu.

adzacita maluwa ngati kakombo, ndi kutambalalitsa mizu yace ngati Lebano. Nthambi zace zidzatambalala, ndi kukoma kwace kudzanga kwa mtengo waazitona, ndi pfungo lace ngati Lebano. Iwo okhala pansi pa mthunzi wace adzabwera, nadzatsitsimuka ngati tirigu, nadzaphuka ngati mpesa, cikumbukilo cace cidzanga vinyo wa Lebano. Efraimu adzati, Ndiri ndi cianinso ndi mafano? Ndayankha, ndidzampenyerera; ndiri ngati mtengo wamlombwa wabiriwiri; zipatso zako zippezeka zocokera kwa Ine. (Hoseya 14:5-8)

MIZU

Mizu imathandiza kuti chomera chikhazikike komanso imaperekera zakudya kuchomera. Salimo 1 imafotokoza mmene munthu angazamitsire mizu ya moyo wauzimu.

WODALA munthuyo wosayenda mu uphungu wa oipa, Kapena wosaimirira m'njira ya ocimwa, Kapena wosakhala pansi pa bwalo la onyoza. Komatu m'cilamulo ca Yehova muli cikondwerero cace; Ndipo m'cilamulo cace amalingima usana ndi usiku. Ndiye akunga mtengo wooka pa mitsinje ya madzi; Wakupatsa cipatso cace pa nyengo yace, Tsamba lace lomwe losafota; Ndipo zonse azicita apindula nazo. (Masalmo 1:1-3)

MPUMULO:

Mpumulo ndi nthawi imene mbeu imakhala ngati yafa chifukwa pamkhala kuti palibe kukula kwina kulikonse. Ndipo izi zimachitika mwakanthawi yokhazikika. Iyi ndi nthawi imene mbeu

imakhala ikupuma ndipo iyi ndi nthawi imene mbeu imakhala kuti yatsala pang'ono kuti ikule kwambiri. Kudziko lakuthupi, Mulungu analamura nthawi yoti nthaka ipumure. (Levitiko 25:5)

Cholinga chimodzi cha ubatizo wa Mzimu Woyera ndi chakuti pakhale mpumuro kapena kutsitsimukanso. Kutsitsimuka kwauzimu kumathandiza kuti pakhale kukula kwa chipatso chauzimu.

Iai, koma ndi anthu a milomo yacilendo, ndi a lilume lina, Iye adzalankhula kwa anthu awa; amene ananena nao, Uku ndi kupuma, mupumitsa wolema, ndi apa ndi potsitsimutsa, koma iwo anakana kumva. (Yesaya 28:11-12)

NTHAKA:

Kuti mutulutse chipatso kudziko lakuthupi ndi lauzimu, nthaka iyenera kukonzedwa moyenelera. Malinga ndi fanizo la ofesa, mmene nthaka inaliri zimakhudza kakulidwe ka mbeu. Kudziko lakuthupi tikhoza Kunena kuti mtima wanu uli ngat nthaka kapena thodi. Ngati mtima wanu ndi ouma komanso odzala ndi zinthu zapadziko lapansi zimene zimatsamwa mau a Mulungu, ndi kovuta kuti mubale chipatso chauzimu.

Ndi udindo wanu kuti mukonze nthaka yauzimu wanu umene ndi mtima wanu kuti ukhale olandira mau a Mulungu:

Mudzibzalire m'cilungamo mukolole monga mwa cifundo; limani masala anu, pakuti yafika nthawi ya kufuna Yehova, mpaka afika Iye, nabvumbitsira inu cilungamo. (Hoseya 10:12)

IMFA:

Pamene mbeu yadzalidwa ndi cholinga choti ibale chipatso, mbeuyo imayenera kufa kaye:

Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Ngati mbeu ya tirigu siigwa m'nthaka, nifa, ikhala pa yokha iyo; koma ngati ifa, ibala cipatso cambiri. (Yohane 12:24)

Wopusa iwe, 8 cimene ucifesa wekha sieikhalitsi'dwanso camoyo, ngati sicifa; (1 Akorinto 15:36)

Moyo wauzimu umatengera kufetsa zinthu zakuthupi. Zinthu izi zimayenera kufa: tchimo, zilakolako zathupi ndi za dziko lapansi. Pamene mwafa kuthupi ndi pamene chipatso cha khalidwe la ngati la Yesu Khristu limakula mkati mwanu.

KUDZIPHATIKA KU MPHESA

Kuti nthambi ibale chipatso imayenera kukhala mbali imodzo ya mtengo. Ngati nthambi yatchoka kumtengo ndekuti nthambiyo singabale chipatso. Yesu Khristu ndi mphesa ndipo ife ndi nthambi. Kuti tibale chipatso, tiyenera kukhala ndi ubale ndi Yesu Khristu.

Ine ndine mpesa weniweni, ndipo Atate wanga ndiye wam'munda. Nthambi iri yonse ya mwa Ine yosabala cipatso, aicotsa; ndi iri y'onse yakubala cipatso, aisadza,

kuti ikabale cipatso cocuruka. Mwakhala okonzeka tsopano inu cifukwa ca mau amene ndalankhula ndi inu, Khalani mwa Ine, ndi Ine mwa inu. Monga nthambi siingathe kubala cipatso pa yokha, ngati siikhala mwampesa; motere mulibe inunso ngati simukhala mwa Ine. Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi zace: wakukhala mwa Ine, ndi Ine mwa iye, ameneyo abala cipatso cambiri; pakuti kopanda Ine simungathe kucita kanthu. (Yohane 15:1-5)

KUTENGULIRA:

Kudziku lakuthupi, mtengo kuti ubale zipatso zambiri, mtengowo umayenera kutenguliridwa. Mlimi amatengulira nthambi zimene sizikubala zipatso ndi cholinga choti nthambizo zibale zipatso zambiri. Mlimi amachotsa nthambi ina iliyonse imene imalepheretsa mtengo kuti ubale.

Kutengulira ndi koyenera pamoyo wauzimu, okhulupirira ametengulidwa ndi chidzudzulo cha Mau a Mulungu. Kutengulira malingana ndi Baibulo kumatchedwa kulanga. Pamene Mulungu watengulira amakhala kuti akuchotsa chinachilichonse chimene chimalepheretsa kukula pamoyo wauzimu. Chifukwa cha ichi, ndikoyenera kuti mutenguliridwe kuti mubale chipatso chazimu.

Nthambi iri yonse ya mwa Ine yosabala cipatso, aicotsa; ndi iri y'onse yakubala cipatso, aisadza, kuti ikabale cipatso cocuruka. (Yohane 15:2)

Nthawi zina anthu sitimatha kupindura ndi zotsatira zakutengulidwa chifukwa chakuti timaona ngati ndi Satana akuchita izi osazindikira kuti ndi Mulungu amene akufuna kuti atikonze. Hoseya akufotokoza cholinga cha chilango kapena kutenguliridwa ndi Mulungu:

Israyeli ndi mpesa wotambalala, wodzibalira wokha zipatso; monga umo zinacurukira zipatso zace, momwemo anacurukitsa maguwa a nsembe ace; monga mwa kukoma kwace kwa dziko lace anapanga zomiritsa zokoma. (Hoseya 10:1)

Zolinga zakutengulira ndi choti munthu abwelere kwa Mulungu. Pamene munthu wabwelera Kwa Mulungu, munthu amayamba kubalanso zipatso za Mzimu Woyera.

NYENGO:

Nyengo ndi chinthu chofunika kwambiri pakakulidwe kachipatso. Kudziko lakuthupi, zipatso zosiyasiyana zimakula mu nyengo zosiyasiyananso. Mwachitsanzo, ngati mungatenge chipatso ndikuchidzala munyengo ina yosiyana ndi nyengo imene chipatsocho chimayenera kudzalidwa, chipatsocho chimafa. Izi zimakhala chomwecho chifukwa cha nyengo zosiyana.

Chimodzimidzi ndi moyo wauzimu, chipatso chathu chiyenera kuonekera munyengo ina iliyonse osati malo ngati kutchalitchi kokha kapena pamene tazungulidwa ndi anthu ena amene amatidziwa.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yoloweza osaonera.

2. Tchulani magawo anayi a mlingo wachipatso chimene chatchulidwa pa Yohane 15.

3. Tchulani zinthu khumi ndi ziwiri zoyenera kuti mtengo wazipatso wachilengedwa ubale chipatso. Dziwani kuti izi ndi zitsanzo zakuthupi zofanana ndi choonadi chazimu chothandiza kuti munthu abale chipatso.

<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>

(mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Werengani nyimbo ya Solomo 4:12 -16. Ndime imeneyi ikupereka chithunzithunzi cha munda wa Mulungu. Anthu ake a Mulungu amene akutchuridwawa ndi mpingo kapena kuti okhulupirira. Moyo wanu ndi nthaka yauzimu imene ikhoza kubala chipatso chauzimu, tchire, kapena nthakayo ikhoza kukhala opanda kanthu. Kodi ndi chiani chimene chikumera mu nthaka ya moyo wanu wauzimu? Kodi munthaka yauzimu wanu muli tchire ndi minga za:

- Nkhawa ndi kusamala zinthu zadziko lapansi?
 - Kunamiza kwa chuma?
 - Chilakolako cha zinthu zadziko lapansi?
1. Kodi ndi chiani chimene chimatenga nthawi yambiri ya moyo wanu? Kapena ndi chiani chimene chimatenga nthawi ndi chidwi chanu? Kodi ndi chiani chimene chili chofunika kwambiri pa zinthu zanu? Kodi munda wantima wanu ndi wamiyala? Kodi muli ndi mtima wa mwala mmagawo amene simumafuna kumvera malamuro a Khristu Yesu ndi magawo amene ali osabala kapena kuti nthaka yauzimu yopanda kanthu.
 2. Phunziro ili ndi lomaliza mumaphunziro a Utumiki wa Mzimu Woyera. Kuti muphunzire zambiri, ndikoyenera kuti mupeze phunziro lina la Harvestime International Institute yotchedwa “ndondomeko zauzimu: Mlozo wankhondo yauzimu.” Phunziro limeneli limafotokoza za ntchito ya Mzimu Woyera pa nkondo yauzimu komanso udindo wa MulunguTate ndi Mulungu mwana.
 3. Malizitsani kauniuni wa chipatso chauzimu. Kuyankha mafunso awa moona mtima ndikofunika chifukwa izi zikuthandizani kuti mudziwe mlingo wachipatso chauzimu mmoyo wanu.

KAUNIUNI WA CHAPATSO.

Werengani ziganizo zili munsimuzi ndipo sankhani nambala imene mukuona kuti ikufotokoza mlingo wachipatso chanu chauzimu. Yankhani funso lina lilironse polemba nambala. Mwachitsanzo mukhoza kulemba 2,3,1 kapena 0.

3 Akutathauza kuti chipatsocho chikuonekera mmoyo wanu.

2 akutanthauza kuti chipatsochi chimaonekera mmoyo wanu nthawi zambiri zina.

1 akutanthauza kuti chipatso chimaonekera mmoyo wanu apo ndi apo.

0 akutanthauza kuti chipatso sichimaonekera mmoyo wanu.

Chitsanzo: _2_1 Ndili ndi chilitsikimikizo kuti tsogolo langa liri mmanja mwa Mulungu.

(Munthu amene anayankha funso ili analemba 2 amene akutanthauza kuti zimene zalambadwa pamwambazi zimaonekera nthawi zambiri mwa munthu ameneyu.

- ___1 Ndili ndi chitsikimizo kuti tsogolo la moyo wanga liri mmanja mwa Mulungu.
- ___2 Ndikudziwa ngati Yesu mwa iye yekha anakwanitsa kuchita chifuniro cha Mulungu.
- ___3 Ndikugwirizana nazo kuti Chikhulupiriro changa chikhoza champhamvu ngati Mulungu ndi okhukupulira.
- ___4 Ndikudikira kukwaniritsidwa kwa malonjezano a Mulungu.
- ___5 Nthawi zina ndimaona ngati Mulungu wakwiya.
- ___6 Ndikuzindikira kuti chisomo cha Mulungu choonetseredwa kudzera mwa Yesu Khristu chinandipulumutsa kuchilango chimene chimayenera ine.
- ___7 Ndine oyamika kwambiri kuti Mulungu amapereka mwana wake obadwa Yekha Yesu Khristu.
- ___8 Ndikudziwa kuti kupezeka kwa Mulungu ndi chimwemwe changa.
- ___9 Ndimagwirizana nazo zimene Mulungu samafuna komanso kutsutsana nazo zimene Iye amatsutsana nazo
- ___10 Ndikuvonereza kuti Yesu analonjeza mtendere.
- ___11 Ndine okonzeka kukhala pansu pa ulamuliro wa Yesu mmoyo wanga.
- ___12. Ndikukhulupirira kuti Yesu ali yemweyo dzulo, lero kufikira muyaya.
- ___13. Ndikutha kuzindikira zofooka za anthu ena pozindikira kuti Mulunguakuchita naobe.
- ___14. Ndine otsikimikizika ndi Mulunguwambino komanso olanga.
- ___15. Ndimakhulukira anthu ena chifukwa Yesu anandikhulukira.
- ___16. Ndimadziwa kuti Mulungu amandikonda ngakhale sindimakonda anthu ena.
- ___17. Ndili ndi chitsikimizo chachipulumutso polandira Yesu Khristu ngati Mbuye.
- ___18. Ndikuphonzira kukana zinthu zazing'ono kuti ndikumane ndi zinthu zazikulu za Mulungu.
- ___19. Ndili ndichitsikimizo chachikhulukiro chamachimo.
- ___20. Ndikudzipereka ndekha ku Mau a Mulungu komanso Mzimu Woyera.
- ___21. Ndimakhulupirika pokwaniritsa malonjezano anga.
- ___22. Ndimapirira pamene ndikumana ndi nyengo zovuta, kukhumudwitsidwa komanso chizuzo.
- ___23. Ndimachita zinthu zanga malingana ndi Baibulo tsiku ndi tsiku.

- ___24. Ndimatonthoza, kulimbikitsa ndikupereka uphungu kwa anthu ena.
- ___25. Ndimathandiza zosowa za abale anga ndi anzanga opanda kuyanga'nira nyengo.
- ___26. Ndikukula ndi kukhwima monga mmene Mulunguamafunira.
- ___27. Ndimakhala ndi nthawi yokhazikika yolumikizana ndi Mulungupandekha.
- ___28. Ndili ndi chikhulupiriro kuti ndine wangwiro pamaso pa Mulungu.
- ___29. Ndimakonetsera kuphunzitsika, kudzichepetsa komanso kugwira ntchito ndi anthu ena.
- ___30. Ndine odalirika povomera udindo wanga wopatsidwa.
- ___31. Ndikudikira Kuti Mulunguandithandize kukhala chimene iye akufuna.
- ___32. Ndimakhulupirika ponena chilungamo, komanso kusunga malonjezano anu.
- ___33. Ndimayankhula mau omangilira anthu ena.
- ___34. Ndimazindikira ubwino wa anthu ena ngakhale akutsutsa nane.
- ___35. Ndimakhutitsidwa ndi kuchita chifuniro cha Mulungu.
- ___36. Ndimagwira ntchito limodzi ndi anthu ena ndi cholinga choti andithandize zinthu zofooka pamoyo wanga
- ___37. Ndili ndi mtendere mkati mwanga chifukwa ndinalora Mzimu Woyera kuti alamulire moyo wanfa.
- ___38. Ndimavomeleza maganizo a anthu ena ndi cholinga choti ndikonze zinthu zimene ndikulakwitsa.
- ___39. Ndikuchita bwino malinga ndikuthekera kumene ndili nako.
- ___40. Ndayamba ndaimitsa kaye zinthu zina zonse zongosangalatsA kuthupi ndi cholinga choti ndikule moyo wauzimu.
- ___41. ndimadzudzula anthu ena pamene akusemphana ndi chifuniro cha Mulungu.
- ___42. Ndimamvetserandi cholinga kuti ndimvetsetse anthu ena.
- ___43. Ndimatumikira anthu amene sanganditumikire ine.
- ___44. Ndimakondwera ndi zinthu zauzimu zimene ndimakwaniritsa.
- ___45. Ndimachita zinthu moyenera ndi cholinga choti ndikonze mavuto okhudza zinthu zokhudza ndalama, kugonana ndi miseche.
- ___46. Ndimadzigwira ngakhale ndikhale ndikusemphana ndi anthu ena.
- ___47. Ndimadzichepetsa mu zinthu zimene ndimakamba.
- ___48. Ndimasamala ndalama, nthawi komanso ine mwini pozindikira kuti ndi Za Mulungu.
- ___49. Ndimakhalabe ndi chiyembekezo ngakhale ndikumane ndi zowawa.

- __50. Nyali yanga kapena kuwala kwanga kumaonekera kwa anthu ena kudzera mu ntchito zabwino.
- __51. Ndimatha kuona chosowa ndikuthandiza moyenera.
- __52. Ndinakhulukira anthu onse amene anandilakwira.
- __53. Ndimapeza chimwemwe ndi zimene Mulunguakuchita mmoyo wakhulupilira.
- __54. Mtima wanga sumavutika ndi mkawa zadziko lapansi.
- __55. Ndimapewa kubweza choipa pamene ena andilakwira.
- __56. Ndikhoza kudalilika mu nthawi ya zowawa.
- __57. Ndimavomeleza anthu ena amene akuchita bwino kuposa ine mmagawo ena.
- __58. Ndimakhala gawo limodzi lolimbana ndi kusowa chilungamo.
- __59. Ndimatha kuchita ubale ndi anthu ena amene anthu ena amati akuchita zinthu zimene ndi zauchimo.
- __60. Ndimapephelera adani anga ndi anthu onse osandikonda.
- __61. Ndimakondwera pamene ndakwaniritsa ntchito yautumiki.
- __62. Ndimapewa nyengo zimene ndikhoza kuyesedwa mosavuta.

KAPEZEDWE KA MALIKISI

1. Lembani mayankho anu amafunso amene mwayankha pamwambapa. Mwachitsanzo, yankho lanu la fuso 1 linali “3”, Lembani 3 mukabokosi koyamba.
2. Pamene mwamaliza kulemba mafunso mmabokosi, okhetserani mayankho onse amene mwalemba.

⇒	⇒	⇒	⇒	⇒	⇒	⇒	Zonse pamodzi
1	10	19	28	37	46	55	Mtendere
2	11	20	29	38	47	56	Kudzichepetsa
3	12	21	30	39	48	57	Chikhulupiro
4	13	22	31	40	49	58	Chipiro
5	14	23	32	41	50	59	Chifundo
6	15	24	33	42	51	60	Chifatso
7	16	25	34	43	52	61	Chikondi
8	17	26	35	44	53	62	Chimwemwe
9	18	27	36	45	54	63	kudziletsa
					234		

KAGWIRITSIDWE NTCHITO KA KUNIUNI

Malinga ndi zotsatira za kauniuni wachipatso chauzimu, malizitsani zinizo izi:

1. Wonani gawo limene magawo amene simunachite bwino, kenako malizitsani ziganizo izi:

Kauniuni akuonetsa kuti ndikuyenera kukuza chipatso cha:

-
2. Ndasankha chipatso chimodzi choti mapemphero anga akhazike pachipatso chimenechi kwa mwezi wathunthu. Chipatso chimenechi ndi: _____
 3. Kuonjezera pemphero, ndipanga zinthu izi kuti zindithandizire kukuza chipatso chimenechi. Onani chipatso chimodzi kenako malizani chiganizo chimenechi.

__ Ndiyamba kupanga chinachake chatsopano.

Kodi muyamba kuchita chiani? _____

___ Ndisiya kuchita chinachake chimene ndikupanga pano.

Ndichiyani chimene musiye kupanga. _____

___ Ndisintha chinachake mmoyo wanga.

Ndichiani chimene musinthe? _____

ZINTHU ZINA ZAPADERA

Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; kuti akonzere oyera mtima: ku nchito ya utumiki, kumangirira thupi la Kristu; kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa cikhulupiriro, ndi wa cizindikiritso ca Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa cidzaloca Kristu. Kuti tisakhalenso makanda, ogwedezekagwedezeka, natengeka-tengeka ndi mphepo yonse ya ciphunzitsi, ndi tsenga la anthu, ndi kucenjerera kukatsata cinyengo ca kusoceretsa; koma ndi kucita zoonza mwa cikondi tikakule m'zinthu zonse, kufikira iye amene ali mutu ndiye Kristu; kucokera mwa Iye thupi lonse, lokowanidwa ndi lolumikizidwa pamodzi, pothandizanapo mfundo yonse, monga mwa kucitisa kwa ciwalo conse pa muyeso wace, licita makulidwe a thupi, kufikira cimango cace mwa cikondi. Pamenepo ndinena ici, ndipo ndicita umboni mwa Ambuye, kuti simuyendanso inu monganso amitundu angoyenda, m'citsiru ca mtima wao, (Aefeso 4:11-17)

mucerezane wina ndi mnzace, osadandaula: monga yense walandira mphanso, mutumikirane nayo, ngati adindo okoma a cisomo ca mitundu mitundu ca Mulungu; akalankhula wina, alankhule ngati manenedwe a Mulungu; wina akatumikira, acite ngati mu mphamvu imene Mulunguampatsa, kuti m'zonse Mulungualemekezidwe mwa Yesu Kristu, amene ali nao ulemmerero ndi mphamvu ku nthawi za nthawi. Amen. 1 Petro 4:9-11

Pakuti monga m'thupi limodzi tiri nazo ziwalo zambiri, ndipo ziwalo zonsezo siziri nayo nchito imodzimodzi; comweco ife, ndife ambiri, tiri thupi limodzi mwa Kristu, ndi ziwalo zinzace, wina ndi wina. Ndipo pokhala ife ndi mphanso zosiyana, monga mwa cisomo copatsidwa kwa ife, kapena mphanso yakunenera, tinenere monga mwa muyeso wa cikhulupiriro; kapenayakutumikira, tidzipereke ku utumiki uyu; kapena iye wakuphunzitsa, kukuphunzitsako; kapena iye wakudandaulira, kukudandaulirako; wakugawira acite ndi mtima wona; iye wakuweruza, aweruze ndi cangu; iye wakucita cifundo, acite ndi kukondwa mtima. (Aroma 12:4-8)

Koma za mphanso zauzimu, abale, sindifuna kuti mukhale osadziwa. Ndipo pali mphanso zosiyana, koma Mzimu yemweyo. Ndipo pali mautumiki osiyana, koma Ambuye yemweyo. Ndipo pali macitidwe osiyana, koma Mulungu yemweyo, wakucita zinthu zonse mwa onse. Koma kwa yense kwapatsidwa maonekedwe a Mzimu kuti apindule nao. Pakuti kwa mmodzi kwapatsidwa mwa Mzimu mau a nzeru; koma kwa mnzace mau a cidziwitso, monga mwa Mzimu yemweyo: kwa wina cikhulupiriro, mwa Mzimu yemweyo; ndi kwa wina mphanso za maciritso, mwa Mzimu mmodziyo; ndi kwa wina macitidwe a mphamvu; ndi kwa wina cinenero; ndi kwa wina cizindikiro ca mizimu; kwa wina malilime a mitundu mitundu; ndi kwa wina mamasulidwe a malilime. Koma zonse izi acita Mzimu mmodzi yemweyo, nagawira yense payekha monga afuna. Koma tsopano, Mulungu anaika ziwalo zonsezo m'thupi, monga anafuna. Koma tsopano pali ziwalo zambiri, koma thupi limodzi Akorinto (Mavesi osakhika ochokera pa 1 Akorinto 12)

MAYANKHO AMAFUNSO ODZIYESA NOKHA

1. Ndipo Yesu, pamene anabatizidwa, pomwepo anaturuka m'madzi: ndipo onani, miyamba inamtsegukira Iye, ndipo anapenya Mzimu wa Mulunguwakutsika ngati nkhunda nudza nutera pa Iye; ndipo onani, mau akucokera kumiyamba akuti, Uyu ndiye Mwana wanga wokonedwa, mwa Iyeyu ndikondwera. Tate, Mwana ndi Mzimu Woyera.
(Mateyu 3:16-17)
2. Mzimu Woyera ali ndi maganizo.
 - Amasanthula mitima ya anthu.
 - Ali ndi chifuniro.
 - Amalankhula.
 - Amakonda
 - Amapembedzera.
3. Izi zikuthanthauza kuti iye amakhudzika ndi zimene munthu amachita.
4. – kunama kwa Mzimu Woyera.
 - kukana Mzimu Woyera.
 - Kuzima Mzimu.
 - Kuliritsa Mzimu.Woyera.
 - Kutukwana Mzimu Woyera.
 - Kunoza Mzimu Woyera.
 - Kukwiyitsa Mzimu.
5. 5,3,2,1,4

CHAPUTALA 2

1. Kodi simudziwa kuti muli Kacisi wa Mulungu, ndi kuti Mzimu wa Mulunguagonera mwa inu? Chizindikira chimene chimaimira chinthu china. Ndi chizindikirop chimene chimene chimakhala ndi tanthauzo lapadera. (1 Akorinto 3:16)
2. 5,4,3,1,2.
3. -Kupezeka kwa Mulungu.
 - Chivomerezo.
 - chitetezo kapena chitsogozo.
 - kuyeretsa.
 - Mphatso ya Mzimu Woyera.

- Chiweruzo.
- 4. - Mzimu wa Mulungu.
 - Mzimu wa Khristu
 - Mzimu wamuyaya.
 - Mzimu wachoonadi
 - Mzimu wachisomo.
 - Mzimu wamoyo.
 - Mzimu wa ulemero.
 - Mzimu wa luntha kapena luntha ndi mavumbulutso.
 - Mtonthozi.
 - Mzimu wamalonjezano.
 - Mzimu wachiyero.
 - Mzimu wachikhulupiriro
 - Mzimu waumwana.

CHAPUTALA. 3

1. KomaNkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m'dzina langalyeyo adzaphunzitsa Inu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu (Yohane 14:26).
2. - Anatsikira pakati pa atsogoleri Israeli.
 - Anatsikira mmalo awo opembedzera.
 - Anawatsogolera k 16:7-11 lupita ku dziko lamalonjezano.
 - Adzafika pakati pa Israeli munthawi ya Mazuzo.
 - Adzafika pakati pa Israeli munthawi Ya Ulamuliro wa Yesu wa dzaka chikwi.
3. Zoonu.
4. 2,1,3.
5. Yohane, 16:7-11
6. Mzimu Woyera amachepetsa kapena kubweza mphamvu ya Satana.
7. - Yesu anali.
 - Abadwa kudzera mwa Mzimu Woyerea.
 - Anadzodzedwa ndi Mzimu Woyera.

- Anazindikiridwa ndi Mzimu Woyera.
- Kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera.
- Kulimbikitsidwa ndi Mzimu Woyera.
- Kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera.
- Osautsika mkati mwa mzimu wake.
- Anakondwera mwa Mzimu Woyera.
- Anaperekedwa kudzera mwa Mzimu Woyera.
- Anauka kwa akufa kudzera mwa Mzimu Woyera.
- Anawalamulira ophunzira kudzera mwa Mzimu Woyera.

8. Mzimu Woyera.

- Anachipanga icho.
- Amathandiza kupembedzera.
- Amatsogoza pa ntchito yotumikira mau a Mulungu.
- Amasankha atimiki.
- Amadzodza alaliki.
- Amapereka chitsogozo popanga chiganizo.
- Amabatiza mmadzi.

9. Mzimu Woyera:

- | | |
|--|------------------------------|
| - Amatsutsa. | |
| - Amayeretsa. | |
| - Amakhala mkati mwathu. | -amalimbikitsa |
| - Amathandiza kuti tifanane naye Yesu Khristu. | -amapembedzera |
| - Amayanjanitsa. | - Amaonetsera choonadi |
| - Amatsogoza. | -amavumbulutsa choonadi |
| - Amapereka chitsogozo chachipulumutso. | -Amaphunzitsa |
| - Amapereka ufulu. | -amalankhula kudzera mwa iye |
| - Amatithandiza kuti tichitire umboni za Yesu. | -amatonthoza |
| - Amaonetsera mphamvu ya Mulungu. | -amapereka machiwa. |

10. Anakhala mboni za mphamvu a Uthenga wambwino wa Yesu Khristu Machitidwe.

CHAPUTALA 4

1. Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. Macitidwe 1:8
2. - Lapani ndikubatzidwa.
 - Khulupirirani kuti ndi wainu.
 - Muyenera kuonetsa kufuna.
 - Vomerezeni kuti ndi mpatso.
 - Lolerani kapena gonjerani Mulungu.
 - Pemphani mapemphero a Khulupilira ena.
3. Kulankhula mu chilankhula chosadziwika kwa amene akulankhula.
4. Amalimbikitsa okhulupilira kuti achitire umboni wa Uthenga Wabwino. Machitidwe 1:8.
5. - Okhukulupirira wina aliyense amalandira Mzimu Woyera pamene wabadwa mwatsopano.
 - Baibulo limafotokoza kuti sionse amalankhula mmalilime.
 - Mantha.
6. Ayi.
7. Kumiza chinthu chonse.
8. – Machitidwe 2:2-4.
 - Machitidwe 10:44-46
 - Machitidwe 19:6.

CHAPUTALA 5.

1. Koma za mpatso zauzimu, abale, sindifuna kuti mukhale osadziwa. (1 Akorinto 12:1)
2. Luso ndi kuthekera kumene munthu amabadwa nako kapena luso limene limakula kudzera mudzikunzekeletsedwa. Pamene mpatso yauzimu ndi kuthekera Mzimu Woyera amapereka. Mpatso yauzimu munthu samabadwa nayo kapena kuyikuza kudzera kuphunzira kapena kukonzekera. Iyi ndi mpatso yapadera imene Mzimu Woyera amapereka.
3. - Oyera mtima angwira.
 - Kulimbitsa ntchito yautimiki.
 - Kuthandizira thupi la Khristu.
4. - Tidzakwanitsa:

- Kukhala oyanjana muchikhulupiro.
 - Kukuza chidziwitso chanthu mwaYesu.
 - Kuti tikhazikike komanso tisanyengedwe ndi ziphunzitso zonyenga.
 - Kukhwima muuzimu mwa Yesu.
5. Inde. Yes. I Petro 4:10 ndi I Akorinto 12:7 ndi 11.
 6. -posagwiritsa ntchito mphatso zimene muli nazo.
 - Kufuna kugwiritsa ntchito zimene mulibe.
 - Kugwiritsa ntchito mphatso mosenera.
 - Kutamandira mphatso yanu.
 7. Mzimu Woyera.
 8. Chikondi. I Akorinto 13.
 9. Mphatso zachinyengo sizimakwaniritsa zolinga za mpatso zauzimu zimene zaperekedwa pa Aefeso 4: 12-15. Sizimagwirizana ndi zimene Baibulo limaphunzitsa zokhudza Yesu. Anthu amene ndi achinyengo amaonetsera makhalidwe amene akufotokokozeredwa pa II Petro 2 ndi Yuda.
 10. Mphatso zauzimu ndi kuthekera kwauzimu kumene kumaperekedwa ndi Mzimui Woyera kwa okhulupirira ndi cholinga kuti achite bwino moyenera.
 11. Mphatso zonse zauzimu ndi zoti zigwire ntchito lero lino chifukwa cholinga chimene mpatsonzi zinaperekedwera sizinakwanilitsidwe. Mphatso zauzimu zikhala zikugwira ntchito kufikira tsiku limene okhulupilira adzakhale agwiro. Izi zikuthandauza kuti kifikira nthawi imene Yesu adzakhazikitse Ufumu wake pa dziko lapansi.
 12. Mpatso ya Mzimu Woyera inaperekedwa pa tsiku la Pentekoste ndipo mphatsozi ndi kuthekera kwauzimu kumene amakhala nako.
 - a. T
 - b. F
 - c. F
 - d. F
 - e. F
 - f. T
 - g. T
 - h. T
 - I. T

CHAPUTALA 6.

1. Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; (Aefeso 4:11)
2. - Atumwi.
 - Aneneri.
 - Alalaliki
 - Abusa
 - Aphunzitsi.
3. Chifukwa chakuti mphatso ndi mphatso yapadera ya utsogoleri mu mpingo.
4. a. Zoona, b. Zoona. C. Zoona.
5. 2,1,4,3,5.
6. -Mphatso zapadera.
 - Mphatso zokhudza kulankhula
 - Mphatso zotumikira
 - Mphatso za zozizwitsa.

CHAPUTALA 7

1. Koma tsopano, Mulungwanaika ziwalo zonsezo m'thupi, monga anafuna (1Akorinto 12:18).
2. - Uneneri.
 - Kuphunzitsa.
 - ulimbikitsa.
 - Mau a Mzeru
 - Mau a chidziwitso.
3. 2,1,4,3,5
4. C.
5. Zabodza.

CHAPUTALA 8.

1. Ndipo amene ali yense afuna kukhala woyamba mwa inu adzakhala kapolo wa onse (Marko 10:44)
2. – Kuzindikira mizimu.

- Utsogoleri.
 - Kuyendetsa zinthu.
 - Chikhulupiriro
 - Kupereka
 - Kuthandiza
 - Kutumikira
 - Chifundo
 - Kucheleza alendo
3. Amathandiza kupereka dongosolo komanso ndondomeko mumagawo auzimu ndi amoyo.
 4. Munthu amene ali ndi mphatso yakayendetsedwe kazinthu ali ndi kuthekera kotsogolera, kukonza zinthu ndi kupanga ziganizo mmalo mwa anthu ena. Mphatso yautsogoleri imathandiza kukopa anthu ena kuti akwaniritse zolinga kapena zofuna kubweretsa ulemelero kwa Mulungu.
 5. Kutumikira kumasiyana ndi kuthandiza chifukwa kutumikira kumamupepuza munthu wina ku udindo wake. Munthu amene akutumikira amakhala kuti wasenza udindo ochita chinachake ndi cholinga choti apereke mwai kwa anthu ena kuti akwaniritse kugwiritsa ntchito mphatso zao.
 6. 9,6,2,3,5,7,11,4,8.
 7. Zabodza.
 8. Tanthauzo la chikhulupiriro laperekedwa pa Aheberi 11:1.
 9. Mphatso ndi mphamvu. Chipatso ndi chikhalidwe.
 10. Pakumvera mau a Mulungu. Aroma 10: 17.

CHAPUTALA 9.

Tidzapulumuka bwanji ife, tikapanda kusamala cipulumutso cacikuru coteri? cimene Ambuye adayamba kucilankhula, ndipo iwo adacimva anatilimbikitsira ife; pocita umboni pamodzi nao Mulungunso ndi zizindikilo, ndi zozizwitsa ndi mphamvu za mitundu mitundu ndi zogawira za Mzimu Woyera, monga mwa cifuniro cace (Ahebri 2:34)

- Zozizwitsa.
- Machiritso
- Malilime.
- Kumasulira malilime.

1. Ndipo zizindikilo zina zambiri Yesu anazicita pamaso pa akuphunzira ace, zimene sizinalembedwa m'buku ili; koma zalembedwa izi kuti mukakhulupirire kuti Yesu ndiye Kristu Mwana wa Mulungu, ndi kuti pakukhulupira mukhale nao moyo m'dzina lace. (Yohane 20:30-31)
2. 2,3,4,1
3. a.F; b.T; c.F; d.F; e.T; f.F; g.F; h.F.

CHAPUTALA 10:

1. zimenezo, ena pozilambalala anapatukira kutsata mau opanda pace; – Kukwaniritsa zolinga ndi zofuna kukwaniritsa. (1 Timoteo 1:6)
 - Kumenya nkhondo yauzimu.
 - Kuti musazunzidwe.
 - Kuti musakhumudwe.
 - Kuti mutenge udindo.
2. Njira 1: Kubadwa mwatsopano.
 Njira 2: Kulandira ubatizo wa Mzimu Woyera.
 Njira 3: Kuzindikira mphatso zauzimu:
 Njira 4: Kuyanga'anira anthu ena amene ali ndi mphatso zauzimu.
 Njira 5: Kufunafuna mphatso zauzimu.
 Njira 6: Kusanjikidwa manja.
 Njira 7: Kuunikila zinthu zauzimu zimene mumakonda.
 Njira 8: Mtsogoleri wauzimu aunikire za mpatso zanu.
 Njira 9: Unikira utumiki wanu wakale.
 Njira 10: Yankhani mafunso okhudza mphatso zauzimu.
 Njira 11: Pezani mphatso zauzimu zimene mukuona kuti Muli nazo.
 Njira 12: Pezani zosowa zauzimu.
 Njira 13: Kwaniritsani zosowa zauzimu:
 Njira 14: unikirani mphatso zanu zauzimu.

CHAPUTALA 11:

1. Kulalikira uthenga Wabwino, kukhala mboni yamphamvu ya Uthenga Wabwino.
2. Chipatso cha Mzimu chamkati cha makhalidwe ngati Yesu Khristu.
3. (Agalatiya 5: 22-23)

- Chikondi - Chimwemwe
 - Mtendere - Chipiriro
 - Chifatso - Chifundo
 - Chikhulupiriro Kudzichepetsa
 - Kudziletsa
4. Yohane 15:16.
 5. Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, icikhulupirtro, cifatso, ciletso; pokana zimenezi palibe lamulo. (Agalatiya 5:22-23)
 6. Chipatso cha Mzimu Woyera ndi chofunika chifukwa sizokwanira kukhala ndi maonekedwe achipembedzo. Ndikoyenera kukhala ndi chipatso chifukwa izi zimaonetsera kuti ndife ake a Mulungu. Chipatso chimakhala ndi mbeu yoti tibale mudziko lauzimu.
 7. Mtendere ndi Mulungu umapezeka pamene talungamitsidwa kudzera mukukhulukidwa kwa machimo athu. Mtendere wa Mulungu umalandiridwa pamene tabadwa mwatsopano. Uwu ndi mtendere umene Mulungu amapereka tsiku ndi tsiku la moyo wathu (werengani Aroma 5:1 ndi Afilipo 4:7)

CHAPUTALA 12.:

Ndipo nchito za thupi zionekera, ndizo dama, codetsa, kukhumba zonyansa, kupembedza mafano, nyanga, madano, ndeu, kaduka, zopsa mtima, zotetana, magawano, mipatuko, njiru, kuledzera, mcezo, ndi zina zotere; zimene ndikucenjezani nazo, monga ndacita, kuti iwo akucitacita zotere sadzalowa Ufumu wa Mulungu. (Agalatiya 5:19-21)

1. Ntchito zakuthupi.
2. Agalatiya 5: 16
3. 17,14,15,16,4,1,2,3,6,5,7,8,13,9,11,10,12.

CHAPUTALA 13:

Nthambi iri yonse ya mwa Ine yosabala cipatso, aicotsa; ndi iri y'onse yakubala cipatso, aisadza, kuti ikabale cipatso cocuruka. (Yohane 15:2)

1. Chipatso, zipatso zambiri, zipatso zochulukira, chipatso chokhazika.
2. Moyo, Madzi, kuwala, malo, mizu, kupumula, imfa, kuphatikizidwa ku mphesa, kutengulira, nyengo.